CHIYAMBI CHA KUPEMBEDZA KWA CHIKHRISTU

shepherds
GLOBAL CLASSROOM

CHIYAMBI CHA KUPEMBEDZA KWA CHIKHRISTU

shepherds
GLOBAL CLASSROOM

Umwini wa Kukopera © 2023 Shepherds Global Classroom
Lotanthauzidwa mu [Chichewa] chochokera [Masulira koyamba/Kwachiwiri] ku kusindikiza [English].
Lopezeka pa kutsitsa mwa ulere pa https://www.shepherdsglobal.org/downloads

Phunziro ili lapezeka pansi pa chiphanso cha Creative Commons Attribution-NonCommercial-NoDerivatives 4.0 International License (CC BY-NC-ND 4.0) kupatula pena patadziwika mwa njira ina. https://creativecommons.org/licenses/by-nc-nd/4.0/

Maphunziro awa akhoza kuchulukitsidwa ndi kugawidwa mwa ulele posindikizidwa komanso kugawidwa pa kompyuta koma osasintha zolemba za mkatimu mwanjira ina iliyonse komanso silikuyenera kugulitsidwa mopeza phindu (ngakhale kuti mtengo wosindikizira ukhoza kuikidwa). Malo ochitira maphunziro ali omasuka kugwiritsa ntchito/kukopera phunziro ili ngakhale ataika mtengo olipilira maphunziro. Mukafuna kudziwa zambiri, chonde onani pa tsamba la www.shepherdsglobal.org/copyright

Zolembedwa zotengedwa kwina ndi za umwini wa kukopera ochokera kwa eni ake ndikugawidwa pansi pa ziphaso zosiyasiyana.

Kupatulako zitanenedwa, malemba onse atengedwa mu Mawu A Mulungu Mu Chichewa cha Lero. Umwini onse ndi otetezedwa.

Wolemba Wamkulu: Dr. Randall D. McElwain

ZAM'KATIMU

KUONA PHUNZIRO MWACHIDULE 5

1. KUFOTOKOZERA KULAMBIRA 7

2. MULUNGU NDI WOLAMBIRA 29

3. KULAMBIRA MU CHIPANGANO CHAKALE 45

4. KULAMBIRA MU CHIPANGANO CHATSOPANO 67

5. KULAMBIRA MU MBIRI YA MPINGO 89

6. NYIMBO MU KULAMBIRA 105

7. MALEMBA NDI PEMPHERO MU KULAMBIRA 133

8. KUKONZEKERA NDI KUTSOGOLERA KULAMBIRA 161

9. MAFUNSO ENA 187

10. MOYO WA CHIKHALIDWE CHA KULAMBIRA 211

MLOZERA A:NDONDOMEKO ZA KUKONZEKERA MWAMBO WA MAPEMPHERO 224

MLOZERA B: FOMU YOSANTHULA NYIMBO 228

ZOFUNIKA ZOVOMEREZEKA 229

MBIRI YA NTCHITO 231

MALEMBA AMENE AWONDEDWA 232

MAPETO 234

KUONA PHUNZIRO MWACHIDULE

Maphunziro awa amatsogolera ku zofunikira zoyambirira pa nkhani ya kulambira.

Ngati mukuphunzira pa gulu, werengani buku mosinthanasinthana. Muziima mwa kanthawi kuti kalasi ikambirane. Monga mtsogoleri wa kalasiyo mukuyenera kuonetsetsa kuti zokambirana zikulingana ndi zimene mwaphunzira ndizothandiza kukhala ndi malire a nthawi yokambirana.

Mafunso okambirana ndi **Zochitika mkalasi** awonetsedwa polozera pa mfundo yokambirana. Nthawi zonse mukafika pamene pali chimodzi mwa cholozera, muzifunsa (ma)funso lotsatiralo, ndipo ophunzira azikambirana yankho. Yesetsani kuonetsetsa kuti ophunzira aliyense akutenga nawo mbali muzokambiranazo. Ngati ndi koyenera, mukhoza kuitana ophunzirawo aliyense ndi dzina lake.

Malemba ambiri amagwiritsidwa ntchito muphunziro ili. Ndime zoyenera mu kalasi zaonetsedwanso ndi kalozera. Chonde ophunzira ayang'ane mavesi ndi kuwerenga kugulu mosinthana.

Phunziro lililonse limathera ndi **ntchito**. Ntchito ikuyenera imalizidwe ndi kuperekedwa isanafike nthawi ya phunziro lina.

Pali **mayeso** a phunziro lililonse, ameme ali ndi kuloweza malemba. Pamapeto pa kalasi iliyonse, mtsogoleri akhoza kubwereza kuwonanso mafunsowa. Kalasi yotsatira ikamayamba, iyambe ndi mayeso okhudzana ndi mafunso amenewa. Mayeso ayenera kulembedwa posaonera buku lophunzirira, notsi zolembedwa mkalasi, Baibulo, kapena kufunsira kwa ophunzira mzawo. Mayankho a mayeso onse akupezeka ndi mtsogoleri wa kalasi kuchokera mu Kalasi ya Abusa pa Dziko Lonse.

Muphunziro 1, ophunzira amapatsidwa **Ntchito ya masiku 30**. Ntchito imeneyi ikatha, ophunzira aliyense apereke lipoti lachidule kufotokozera zimene waphunzira kuchokera muntchitoyi. Ophunzira sadzapereka mbiri ya zolemba za ntchito yawo.

Ngati ophunzira akufuna **Kulandira setifiketi yochokera ku Kalasi ya Abusa ya Dziko Lonse**, akuyenera kulowa mkalasi ndi kumaliza ntchito. Fomu imaperekedwa pamapeto pa maphunziro pamenepo palembedwe zotulukamo za ntchito yanu ya m'kalasi.

PHUNZIRO 1

KUFOTOKOZERA KULAMBIRA

ZOLINGA ZA PHUNZIRO

1. Kukhala ndi tanthauzo la Baibulo la Kulambira.
2. Kumvetsetsa kuti kulambira kumakhudza madera onse a moyo wathu.
3. Kuzindikira mtundu wa kulambira umene umavomerezedwa ndi Mulungu.
4. Kuyamikira kufunikira kwa kulambira mmoyo wa Chikhristu.

KUKONZEKERA PHUNZIRO ILI

Lowezani Yohane 4:23-24.

CHIYAMBI

Ndi mmawa wa tsiku la Sabata ku America. Akhristu ovala bwino asonkhana kuti alambire Mulungu mu kachisi okongola. Motsatana ndi kwaya komanso limba, akuyimba nyimbo za m'buku. Azitoliro akuyimba pamene chopereka chikuperekedwa. A gulu la matamando akupemphera motsitsa pamene abusa akutsogolera mu pemphero. Panthawi ya ulaliki wawo, abusa akunena mawu a wolemba ochokera mu Laibulare yawo yaikulu. Ulaliki watha, mpingo ukukondwa ndi kudya mgonero pogwiritsa ntchito mbale zokonzedwa ndi siliva, mkate, komanso chikho cha mgonero cha aliyense. Kumeneku ndiko kulambira.

Ndi mmawa wa tsiku la Sabata ku China. Okhulupirira 30 ovala mwawamba asonkhana m'nyumba. Akuimba nyimbo za matamando komanso nyimbo za m'buku koma osagwiritsa ntchito zida. Mtsogoleri akugawa uthenga wa choonadi umene waphunzira posachedwa

kudzera mukuwerenga kwake kwa malemba. Munthawi yowonjezera ya nthawi ya pemphero mamembala nyumba iyi akupemphererana zosowa za wina ndi mzake. Pambuyo pa pemphero, akukondwera mgonero ndi mkate komanso vinyo womwera mu makapu a pulasitiki kupitiriza kwa nthawi ya pemphero, ziwalo za mpingowu zikupemphererana zosowa za wina ndi mzake. Kenako adya mgonero mokondwa pogwiritsa ntchito mkate ndi vinyo akumwera mzikho za pulasitiki. Pamene anthu akuchoka, akupereka chopereka chawo mwakachetechete mu mtanga wa chopereka pafupi ndi anthu. Choperekachi chigawidwa kwa mamembala amene ali ndi zosowa. Uku ndi kulambira.

Ndi m'mawa wa tsiku la Sabata ku Nigeria. A khristu avala zovala zokongola kusonkhanira kulambira kwa mphamvu. Gulu la matamando motsogozedwa ndi magitala, malimba komanso ng'oma akutsogolera nyimbo zowonetsedwa pa nsaru ya kanema. Gulu loyimba likuyimba pamene anthu akuponya chopereka chawo mu chawo mu gome la chopereka kutsogolo kwa tchalitchi. Uthenga ndi odziwika bwino, ukuyankhula ku zosowa za nthawiyo za anthu a ku Nigeria. Mwambo wa mapemphero ukuthera ndi nthawi yopatsana chanza, kukumbatirana, ndi kukondwa. Uku ndi kulambira.

Kulambira kumachitika mmagawo osiyanasiyana. Mdziko lili lonse komanso mchikhalidwe chilichonse, kulambira kumasiyana. Kulambira kumaposa mtundu wina wake wa mwambo wa mkumano. Maka, kulambira kumaposa mwambo pawokha; Kulambira kumakhudza madera onse a moyo wa Chikhristu. Mu phunziro ili tiona kufotokozera kwa Baibulo kwa kulambira.

» Werengani Yohane 4:1-29. Kambiranani tanthauzo la kulambira mumzimu ndi m'choonadi.

MBALI YA KULAMBIRA KWA BAIBULO

Kulambira ndi kulambira kuyenera kwa Mulungu. Kumatanthauza kupereka ulemu kwa Mulungu umene uli omuyenera.

» Mmusimu muli matanthawuzo atatu a kulambira. Lowezani kufotokozera kumene kuli kwa tanthauzo kwa inu.

- "Kulambira ndi m'chitidwe wa kulemekeza kochokera kwa munthu kupita kwa Mulungu wa muyaya. " – Evelyn Underhill
- "Kulambira ndi kukweza mitima yathu mwakufuna kwathu kupita kwa Mulungu." – Franklin Selger
- "Kulambira ndi kuonetsa chimene ife tili ku zonse zimene Mulungu ali." – Warren Wiersbe

Kulambira ndi Kugonjera Kolemekeza

Mawu oyambirira a chi Heberi ndi Giriki otanthauziridwa kuti "Kulambira" mu Baibulo ali ndi mfundo ya kugonjera pamaso pa Mulungu.[1] Izi zikuonetsa kugonjera kodzichepetsa kokhala mu Kulambira. Mchitidwe ogwada mooneka ukuonetsa kulemekeza kwa mtima. Kuyambira zaka mazana aiwiri, Akhristu amagwada ngati kulemekeza akamapemphera.

Chivumbulutso 4:10-11, Mtumwi Yohane anaona kulambira kumene kumachitika kumwamba:

> Izi zikamachitika akuluakulu 24 aja amadzigwetsa pansi pamaso pa wokhala pa mpando waufumuyo, namupembedza wokhala ndi moyo wamuyayayo. Iwo amaponya pansi zipewa zawo zaufumu patsogolo pa mpando waufumu nati: "Ndinu woyeneradi kulandira ulemerero ndi ulemu ndi mphamvu, Ambuye ndi Mulungu wathu, pakuti munalenga zinthu zonse, ndipo mwakufuna kwanu zinalengedwa monga zilili."

Mfumu yogonjetsedwa ikapititsidwa kwa Kaisara, imafunika kuponya chisoti chake cha ufumu pamapazi a Kaisara ndi kugwada mwakogonjera. Yohane akuwonetsa erase kuti Mulungu, amene ali wamphamvu komanso woyenera kuposa Kaisara, amayenera kugonjera kodzichepetsa kwa wolambira.

Mu Chipangano Chakale, Mulungu anakana nsembe ya owukira. Ambuye akuti, "Anthu awa amandipembedza Ine ndi pakamwa pawo, ndi kundilemekeza Ine ndi milomo yawo, koma mitima yawo ili kutali ndi Ine. Kundipembedza kwawo ndi kwa chiphamaso. Amandipembedza motsata malamulo a anthu amene naphunzitsidwa..." (Yesaya 29:13). Kunja, amawoneka ngati olambira; amanena mawu olondola miyambo yoyenera. Mkati mwawo, mitima yawo inali kutali ndi Mulungu. Kulambira koona ndi ugonjera kolemekeza kuchokera mumtima.

Choonadi chomwechi chikuonekanso mu Chipangano Chatsopano. Mzimayi wa ku Samaria anatsutsa za malo akuthupi olambirako, Yerusalemu ndi Phiri la Gerizim. Yesu anakamba za malo akuthupi olambirako, mtima. Mulungu ndi Mzimu, ndipo omupembedza Iye ayenera kumupembedza mu mzimu ndi m'choonadi" (Yohane 4:24). Kulambira koona kumafunika kudzipereka kwa Mulungu.

Kulambira koona kumalemekeza wolambirdwa mmodzi. Mu mipingo ina, kulambira kumalephera kuwonetsera ulemu woyenera kupita kwa Mulungu. Monga mmene tiwonere kutanthawuzira kwa patsogolo, kulambira kumaphatikiza chikondwerero, komanso kulambira kumapereka ulemu kwa Mulungu. Izi sizitanthauza kuti mtundu umodzi wokha

---

1 Mauwa cha Heberi ndi *shachah*, amene amatanthauza kuti "kulambira" "kugwada" "kugwa pansi," kapena. "ulemu." Mauwa mu chi Giriki ndiwo Proskuneo, amene akutanthauza *proskuneo*, amene akutanthauza kulambira" kapena "kugwada" mu Chipangano Chatsopano.

wa kulambira ndiwo woyenera. Komabe, tanthauzo ili limatikumbutsa kuti pamene tipanga chiganizo cha ku lambira, tiyenera kufunsa, “Kodi ndikuwonetsa ulemu kwa Mulungu amene ndimamulambira?”

Kulambira ndi Utumiki

> N’chifukwa chake ine ndikukupemphani abale, mwa chifundo cha Mulungu, kuti mupereke matupi anu monga nsembe yamoyo, yopatulika ndi yokondweretsa Mulungu. Nsembeyi ndiye kupembedza kwanu kwa uzimu (Aroma 12:1).

Vesi ili likulumikiza kudzipereka kwathu kwa ulemu ndi moyo wathu watsiku ndi tsiku. Ndipokhapo pamene tidzipereka monga nsembe yamoyo kuti kutumikira kwathu, kapena kulambira kwathu kuvomerezeke kwa Mulungu. Kukumana pafupipafupi kwa mpingo ndikofunika; mpingo wakale unali kulemekeza Kulambira kwa gulu.[2] Komabe, kulambira sikutha nthawi ya mkumano wagulu. Kulambira koona kumakhudza madera onse a moyo.



Kulambira ndi Kuyamika

Mau akuti *kutamanda* amagwiritsidwa ntchito maulendo 130 mu Buku la Masalimo. Pali mau atatu otathawuzidwa mu Chihebri “kutamanda.” Liwu Loyamba ndipo *halal,* lili ndi tanthauzo la chiganizo cha kukondwera kapena kukweza. Liwu lachiwiri, *yadah,* Limatanthauza kutamanda, kuyamika kapena kuvomereza. Liwu lachitatu, *zamar,* amatanthauza “kuyimba” kapena “kuyimba matamando.”

Mau awa, makamaka akuti *halal,* amapereka ganizo la Chimwemwe cha kulambira. *Halal* amene munthu wachiyuda akhoza kugwiritsa ntchito podzitamandira pamaso pa munthu wina. Mu kulambira timakweza za Mulungu; mu kulambira timakondwelera za ubwino wake; mkulambira timasangalira ukulu wa Mulungu.

Kulambira koona kumalemekeza Mulungu; komanso kulambira koona kumakondwelera Mulungu! Mkulambira timasangalala mu ubwino wa Mulungu. Mu phunziro 6, tidzaphunzira ntchito ya nyimbo mu kulambira. Nyimbo ndi zofunika kwambiri mu kulambira chifukwa zimapeleka njira yoti mpingo uthe kulowa mchisangalalo ndi kumutamanda Mulungu.

---

2 Kulambira kwa kugulu **kulamulidwa** mmalemba monga Aheberi 10:25. Kulambira kwa gulu ndiko **kumaganiziridwa** m’malemba monga Machitidwe 2:46-47.

Kulambira ndi Chiyanjano

Kulambira ndi chiyanjano pakati pa munthu ndi Mulungu. Komanso kulambira kumakhudza chiyanjano pakati pa wolambirawo. Mau a mu chigiriki akuti *koinonia* kutanthauza chiyanjano kapena kugawana amagwiritsidwa ntchito kawirikawiri erase pamene pakukambidwa za kulambira. Akhristu anadzipereka mu chiphunzitso cha atumwi komanso mukuyanjana *Koinonia,* mkunyema mkate ndi mkupemphera (Machitidwe 2:42). Monga wokhulupirira, taitanidwa mu chiyanjano *koinonia* cha mwana wa Mulungu, Yesu Khristu Ambuye wathu (1 Akorinto 1:9).

Chitsanzo cha kuvetsetsera kulambira ndi utatu woyera. Momwemonso monga M'modzi mwa Atatu amayanjanirana wina ndi mzake, timayanjana wina ndi mzake komanso kwa Mulungu erase mukulambira. Mu mdalitso umene amalumikizitsa dziko lapansi ndi utatu wamuyaya, Paulo analemba kuti, "Chisomo cha Ambuye Yesu Khristu, ndi chikondi cha Mulungu, ndi chiyanjano cha Mzimu Woyera zikhale ndi inu nonse" (2 Akorinto 13:14). Monga tili amodzi mwa Khristu, timatenga nawo mbali mu chiyanjano cha Mwana ndi Atate.[3] Mu kulambira, timakumana ndi chiyanjano chachikulu Utatu woyera. Kulambira kwathu kwa dziko lapansi kumachokera pa kuyanjana kwa Utatu woyera.

Kulambira kwa mu Utatu Woyera ndi chisomo, kulambira kumatheka kudzera kwa Wamsembe wathu, Yesu Khristu. Amatenga kulambira kwathu kosayenera, amakuyeretsa, ndipo amakupereka kwa Atate kopanda banga kapena chilema. Kulambira kwathu kumavomelezedwa ndi Mulungu mmalo mwa Yesu, ndipo timakhala amodzi ndi Yesu mmoyo wake wa Uzimu.

Sitilambira chifukwa choti kulambira kumadzetsa kukonderedwa ndi Mulungu, koma chifukwa chakuti, kudzera mu chisomo, tapatsidwa mwayi wokhala nawo m'chiyanjano ndi Mulungu.

Koinonia'*wokhala ndi malire* lero (kuyanjana kwathu ndi Mulungu mu kulambira **ndi** kuyanjana ndi okhulupirira ena) ndi kulawiratu kwa kulambira kwa kumwamba. Monga wolambira, timafuna chiyayanjano ndi okhulupirira chifukwa kulambira padziko ndi kukonzekera kulambira kwa muyaya.

Kulambira Kumakhudza Zonse za Moyo

Liwu lina lokhudza kulambira mu Chipangano Chatsopano nthawi zina limatanthauzidwa kuti "chipembedzo":[4]

> Ngati wina amadziyesa ngati ndi wachipembedzo, koma chonsecho saletsa lilime lake, amadzinyenga yekha ndipo chipembedzo chakecho ndi cha chabechabe.

3 James B. Torrance, *Worship, Community, and the Triune God of Grace* (Downers Grove: InterVarsity Press, 1996), 20-21.

4 Liwu la chi Giriki limalozera za mbali ya kulambira kwa kunja. Machitidwe 26:5, Akolose 2:18, ndi Yakobo 1:26-27.

Chipembedzo chimene Mulungu Atate athu amachivomereza kuti ndi changwiro ndi chopanda zolakwika ndi ichi: kusamalira ana amasiye ndi akazi amasiye pa mavuto awo, ndi kudzisunga bwino kuopa kudetsedwa ndi dziko lapansi (Yakobo 1:26-27).

Mau awa amaonetsa kuti kulambira kumaposera zimene timachita lamulungu. Kulambira kwa Baibulo kumaphatikiza zonse za mmoyo wathu. Mwambo wolambira umakhala ndi chindunji poonetsera kulambira, koma mwambo olambira pawokha siwokwana. Tikuyenera kukhala mmoyo wolambira. Moyo wathu wa sabata iliyonse wolambira limodzi ndi azathu ukuyenera kuwoneka mmoyo wathu wat siku ndi tsiku.



Kulambira kowona kumawoneka mkudzipereka kwathu kwa tsiku ndi tsiku. Yakobo amawonetsa kuti ngati ndiyimba nyimbo zamatamando pa tsiku lamulungu, koma nkumalephera kusankha zoyankhulo pa tsiku lolemba, ndekuti kulambira kwanga Sikuli kokwana. Kulambira koyera komanso kosadetsedwa kumaphatikizapo mwambo wa ku tchalichi (kucheleza ana ndi amayi amasiye) ndi kumvera kwa tsiku ndi tsiku (kudzisunga wekha kukhala opanda banga lochoka ku zamdziko).

Mu Yesaya 6, Mneneri anawona masomphenya a Mulungu ali pa mpando wake wachifumu. Utumiki wa uneneri wa Yesaya unasinthika chifukwa cha masomphenya amenewa. Yesaya anamva Ambuye akufunsa “Kenaka ndinamva mawu a Ambuye akuti, “Kodi ndidzatuma yani? Ndipo ndani adzapite m’malo mwathu?” Ndipo ine ndinati, “Ndilipo. Tumeni!”

» Werengani Malaki 1:6-9, 1 Samueli 13:8-14, Levitiko 10:1-3, ndi Machitidwe 5:1-11. Kodi ndime zimenezi zimaphunzitsa chiyani za kulambira?

N’CHIFUKWA CHIYANI KULAMBIRA KULI KOFUNIKA?

A.W. Tozer anakutcha kulambira “Cha mtengo wapatali chosowa” cha munthawi ino ya mpingo wa makono. Iye anati timadziwa kulalika, timadziwa kuchita usodzi, komanso timadziwa kuchita chiyanjano. Komabe, ndi mphamvu zathu zonsezi, nthawi zambiri timalephera kulambira. Timawonelera mlaliki akulalika; timamvetsera kuyimba kwa kwaya, gulu la matamando, kapena oyimba nyimbo za pawokha akuyimba; timapereka ndalama za chopereka. Koma timalephera kulambira moona; Timalola zochitika za mumpingo kulowa mmalo mwa kulambira.

Kulambira kukuyenera kukhala kofunika kwa ife chifukwa ndikofunika kwa Mulungu.

» Werengani Eksodo 20:1-5 kuti muwone kufunika kumene Mulungu amaika kulambira.

Malamulo awiri oyambirira amakamba zokhudza kulambira. Lamulo loyamba limatiuza **amene tiyenera kumulambira.** "Usakhale ndi milungu ina koma Ine ndekha" (Eksodo 20:3). Lamuro lachiwiri limatiuza **mmene timayenera kulambilira.** "Usadzipangire chofanizira chinthu chilichonse chakumwamba kapena cha pa dziko lapansi kapena cha m'madzi a pansi pa dziko…" (Eksodo 20:4). Kenako, ndime zomaliza za Eksodo 20, Mulungu amabwereranso ku nkhani ya Kulambira. Ndime zimenezi zimaphunzitsa Israeli mmene angamangire guwa la msembe komanso mmene angafikire kuguwali mwa ulemu.

» Werengani Eksodo 20:23-26, Kulambira ndi kofunika kwambiri kwa Mulungu!

Kulambira kumachita gawo lochuluka mu Baibulo. Mabuku a Eksodo ndi Levitiko amapeleka malangizo mwapaderadera okhudzana ndi moyo wa Israeli wa kulambira. Masalimo amatipatsa nyimbo zolambilira. M'mabuku a Uthenga wabwino, timaona anthu akugwada pansi kulambira Yesu.

» Werengani Mateyu 2:11, Mateyu8:2. Mateyu 9:18, Mateyu 14:33, Mateyu 15:25, Mateyu 28:17.

Mu buku la Machitidwe, mpingo ukusonkhana kukalambira.[5] M'makalata ake, Paulo amalankhura za mkhalidwe wolambira mu mpingo (1 Akorinto 11 ndi 1 Timoteo 2). Buku la Chibvumbulutso limatiwuza kuti tiyang'ane kumwamba kuti tiwone kulambira kumene kukuchitika kale kumpando wachifumu wa Mulungu. Kulambira kumene kumachitika padziko lino lapansi ndiko kudzikonzekeretsa kulambira kwathu kwa kumwamba (Chibvumbulutso 4-5). Kulambira ndikofunika kwa Mulungu.

Kulambira Ndikofunika Chifukwa Kudzera mu Kulambira Timaona Mulungu

» Werengani Yesaya 6:1-8. Kambiranani zimene Yesaya anakumana nazo mu Kachisi.

Buku la Yesaya ndime 6 limafotokoza za chithuzithuzi chofunika cha kulambira. Limaonetsa kuti kudzera mukulambira timamuona Mulungu. Mukachisi, ndinawona Ambuye akukwezedwa.

Choonadi ichi chinabwerezedwa mu Malembao monse. Pamene anali kulambira pa tsiku la Ambuye, Yohane anawona masomphenya a kumwamba (Chibvumbulutso 1:10). Panthawi imene Paulo ndi Sila anali kulambira mupemphero ndi kuyimba, Mulungu anawonetsera

5 Akhristu akale anapitiliza kulambira Mulungu mmakachisi, komanso mmasunagoge (Machitidwe 2:46-47, Machitidwe 3:1-11, Machitidwe 5:12,21,42). Kuwonjeza apo, akhristu ena anali kukumana mmakomo mwawo ndikupemphera, kumvera chiphunzitso, ndi kupanga chiyanjano. Izi zonse ndimbali imodzi ya kulambira (Machitidwe 2:46-47, Machitidwe 4:31, Machitidwe 5:42).

mphamvu (Machitidwe 16:25-26). Davide anapilira chizunzo chimene chinamuchititsa iye kulira, “Mulungu wanga, Mulungu wanga, n’chifukwa chiyani mwandisiya? Chifuwa chiyani simukundithandiza ndi pang’ono pomwe? N’chifukwa chiyani simukumva mawu a kudandaula kwanga?” (Masalimo 22:1). Mkatikati mwa chisautso, Davide anamuona Mulungu kudzera mkulambira ndi matamando; “Inu ndinu Woyera, wokhala pa mpando waufumu; ndinu matamando a Israeli” (Masalimo 22:3). Kudzera m’kulambira, timamuona Mulungu.

Kulambira Ndikofunika Chifukwa Kudzera mu Kulambira Timadziwona Tokha Ndipo Timasinthika

M’kachisi, Yesaya sanangoona Ambuye akukwezedwa, anadzionanso iye mwini. Pamene Yesaya anaona Mulungu ali pa mpando wachifumu, anafuula, “Tsono ine ndinafuwula kuti, “Tsoka langa ine! Ndatayika! Pakuti ndine munthu wapakamwa poyipa, ndipo ndimakhala pakati pa anthu a pakamwa poyipa, ndipo ndi maso anga ndaona mfumu Yehova Wamphamvuzonse” (Yesaya 6:5). Kulambira koona kumatipangitsa kudziwona ife eni monga umo Mulungu amatiwonera.

Ichi ndichifukwa chake tikamakamba za pemphero timaphatikiza pemphero lovomeleza machimo. Pemphero lovomeleza machimo silimanena kuti, Tachita kusamvera malamuro a Mulungu ndipo tachita uchimo.” Pemphero lovomeleka limazindikira, “ngakhale mitima ya anthu ambiri amene ali opemphera siyoyera kulingana ndi mmene chiyero cha Mulungu chilili. Timayima Kamba ka chisomo cha Mulungu.”

Pamene tikulambira, timadziwona ife tokha mmene Mulungu amationera. Kupatula kulambira, maonedwe oterewa amakhala opatsa mantha. Komabe, chifukwa choti takumana naye kale Mulungu, timayeletsedwa, osati kutsutsidwa. Chifukwa choti tamuona Mulungu komanso chisomo chake, timadziona tokha moona mtima, timavomeleza njala yathu pa iye, ndipo timapeza chisomo mmoyo wathu.

Kulambira kumaonetsera chimene ife tili, koma sikumatisiya mmene tinalili. Mkuwala kwa chiyero cha Mulungu, Yesaya anadziwona yekha wosalungama. Komabe, mmalo mokhala kakasi, kulambira kunamuthandiza kuti asandulike mtima.

> Ndipo mmodzi wa Aserafi anawulukira pa ine, ali ndi khala la moto mdzanja lake limene anatenga kuchoka pa guwa ndi lilime lake. Ndipo anakhudza pakamwa panga nanena kuti: “Pomwepo mmodzi mwa Aserafi aja anawulukira kwa ine ali ndi khala lamoto m’dzanja lake, khala limene analichotsa ndi mbaniro pa guwa lansembe. Ndipo anandikhudza pakamwa panga ndi khala lamotolo nati, “Taona ndakhudza pa milomo yako ndi khalali; kulakwa kwako kwachotsedwa, machimo ako akhululukidwa” (Yesaya 6:6-7).

Yesaya anasandulika Kamba ka kukumana kwake ndi Mulungu woyera.

Kulambira koona kumamusintha wolambirayo — Yesaya mu kachisi, mzimayi wa ku Samariya pa chitsime paja, komanso Ophunzira a Yesu mu nthawi ya Mawalitsidwe a Yesu Paphiri. Kukumana ndi Yesu kumathandiza kusanduliza munthu wolambira.

Kulambira Ndikofunika Chifukwa Kudzera mu Kulambira Timaona Dziko Lathu

Pakulambira, Yesaya anawona Mulungu; anadziona yekha; anaona zosowa za dziko lake. Tsono ine ndinafuwula kuti, "Tsoka langa ine! Ndatayika! Pakuti ndine munthu wapakamwa poyipa, ndipo ndimakhala pakati pa anthu a pakamwa poyipa, ndipo ndi maso anga ndaona mfumu Yehova Wamphamvuzonse" (Yesaya 6:5). Kenaka ndinamva mawu a Ambuye akuti, "Kodi ndidzatuma yani? Ndipo ndani adzapite m'malo mwathu?" Ndipo ine ndinati, "Ndilipo. Tumeni! (Yesaya 6:8). Mukulambira m'mene ife timakozekeretsedwa ku utumiki wamphavu kudziko losowa.

"Lowani mu Kulambira – Pitani Kukatumikira"

Chizindikiro cha pamwamba pa chitseko la tchaltchi.

Poyambirira, tinaona kuti kulambira koona kumakhudza moyo onse. Mipingo inasiyanitsa kulambira ndi kulalikira. Amati, "cholinga cha mpingo wathu ndi kulalikira. Mipingo ina ikhoza kukhazikika pa kulambira. Kapena akhoza kunena "Cholinga chathu ndi kulambira." Tisiira kulalikira ndi utumwi kwa wina wake. Izi zikuonetsa kusavetsetsa kwa kulambira. Mu kulambira, timalora Mulungu kuti attionetse zosowa zadziko. Kulambira koona kudzathera mu kulalikira.

Kulambira koona kunaonetsera chosowa cha Yesaya — ndipo anasithika ndi kulambira. Kulambira koona kunaonetsera chosowa cha Yesaya — ndipo anadzipereka kusintha dzikolo mu kulambira — tidzapeza kukhudzika kwa kutumikira dziko lathu. Kuvomereza kofunikira kukulambira koona ndi "Ndilipo tumeni."

Oswald Chambers anachnjeza anthu amene amapita ku utumwi, "Ngati simupephera mu zochitika za tsiku ndi tsiku, mukayamba ntchito ya Mulungu, simudzakhala opanda ntchito kokha koma chipsinjo kwa iwo amene ali pafupi ndi inu."[6]

Chambers anazindikira ubwino wa kulambira komanso kukozekera kwa utumiki wamphavu. Mu kulambira, Mulungu amaonetsa zosowa za dziko lotizungilira ndikufikira zosowa zimenezo.

---

6 Oswald Chambers, *Wamkulu Wanga chifukwa cha Ukulu Wake t*, (kulowa kwa September 10). Zatengedwa kuchokera https://utmost.org/missionary-weapons-1/ pa July 21, 2020.

Kulambira Ndikofunika Chifukwa Kulephera kulambira kumatilekanitsa ndi Mulungu

» Werengani Aroma 1:18-25. Kodi pali ubale otani pakati pa kulambira kwabodza ndi chimo?

Kumayambiriro kwa Aroma, Paulo akuonetsa chifukwa chimene munthu amakhalirabe ochimwa pamaso pa Mulungu. Akuonetsa kuti kugwa kwa munthu `ndi zotsatira za kulambira Mulungu owona. Onani ndondomeko imene Paulo akufotokoza pa Aroma 1:21-25:

1. Sanalambire Mulungu. "Ngakhale iwo anadziwa Mulungu, sanamulemekeze ngati Mulungu kapena kumuthokoza, koma maganizo awo anasanduka wopanda pake ndipo m'mitima yawo yopusa munadzaza mdima" (Aroma 1:21). "Iwo anasinthanitsa choonadi cha Mulungu ndi bodza ndipo anapembedza ndi kutumikira zinthu zolengedwa m'malo mwa Mlengi amene ali woyenera kutamandidwa mpaka muyaya. Ameni" (Aroma 1:25).

2. Ngakhale iwo anadziwa Mulungu, sanamulemekeze ngati Mulungu kapena kumuthokoza, koma maganizo awo anasanduka wopanda pake ndipo m'mitima yawo yopusa munadzaza mdima. "Ngakhale ankadzitama kuti ndi anzeru, anasanduka opusa. Iwo anasinthanitsa ulemerero wa Mulungu wosafa ndi mafano opangidwa ndi manja wooneka ngati munthu amene amafa, kapena ngati mbalame, ndi nyama kapena zokwawa" (Aroma 1:21-23).

3. Pa Kuweruza "N'chifukwa chake Mulungu anawasiya kuti azingochita zilakolako zochititsa manyazi zauchimo zomwe mitima yawo inkafuna. Zotsatira zake anachita za chiwerewere wina ndi mnzake kunyazitsa matupi awo..." (Aroma 1:24).

Paulo akuonetsa kuti kugwa kwa munthu mu zopusa, katangale, kusilira zonyasa ngati kukana kulambira Mulungu kwa anthu. Sanalambire Mulungu; analambira ndi kutumikira cholengedwa osati Mlengi.

Aliyense amalambira. Akhristu amalambira Mulungu; A Silamu amapembedza Allah. Munthu wa chikhulupiliro chakuti kulibe Mulungu amalambira nzeru zake. Aliyense amalambira. Ngati tikana kulambira Mlengi, tidzalambira cholengedwa.

Kulambira ndi kofunika. Kulambira kwa Mulungu owona kumatisintha kukhala mu chifanizo chake. Kulambira kwa mulungu wabodza kumatintha kukhala mu chifanizo cha mulungu ameneyo. Timakhala ngati china chilichonse chimene timapemphera.

ZOLINGA ZITATU MU KULAMBIRA

Marva anazindikira zolinga zitatu za Kulambira koona.[7] Mukulambira ti:

1. Mu kulambira timakumana ndi Mulungu.

Mwambo uli onse umene sutibweretsa kwa Mulungu sufikira kukulambira koona. Izi zizitanthauza kuti mwambo ulionse wa kulambira udzakhala wa maimvaimva kapena ochititsa chidwi. Sizitanthauzanso kuti mwambo ulionse udzakhala ndi kulambira monga mwa cholinga chonenedwa. Koma mu mwambo uli onse wa mapemphero, tiyenera tipezeke mu kupezeka kwa Mulungu. Izi zikhoza kukhala kudzera mu choonadi chotengedwa kuchokera mu uthenga; zikhoza kukhala kudzera mu kuwerenga Mawu a Mulungu; zikhoza kukhala mkudzera mu nyimbo zimene zimalemekeza Mulungu; ikhoza kukhala nthawi ya pemphero imene timapezamo mphavu zatsopano pakuyenda kwathu ndi Mulungu. Mwa njira ina, mwambo wa mapemphero uyenera kutibweretsa ife kukumana ndi Mulungu.

2. Mu kulambira timakoza khalidwe la Chikhristu.

Mu kulambira timadziwona tokha ndipo timasinthika. Mu kulambira, timaphunzira choonadi chimene chimasula khalidwe lathu la Chikhristu. Tikamalambira Mulungu, khalidwe lathu limakozeka kukhala mu chifanizo chake. Timakhala ngati china chilichonse chimene timalambira.

3. Mukulambira, timamanga gulu la Chikhristu.

Mu kulambira, timaona dziko lotizungulira ndipo timadzipereka kukutumikira ku zosowa kwa dzikolo. Pamene tichita ichi, mpingo umamangika, ndipo okhulupirira amakula mwa njira iliyonse amene ali mutu, mwa Khristu (Aefeso 4:15). Kulambira koona ndi chida chomangira gulu la Chikhristu loona.

KODI NDI KULAMBIRA KOTANI KUMENE KUMAVOMEREZEKA NDI MULUNGU?

» Kodi ndi mtundu otani wakulambira umene mukuganiza kuti Mulungu amavmereza?

Yesu anauza mzimayi wa ku Samariya kuti olambira oona amamulambira iye mumzimu ndi m'choonadi (Yohane 4:23-24). Pali kulambira koona kumene kumavomerezeka kwa Mulungu; izi zikuonetsa kuti pali kulambira kwabodza kumene sikuvomerezedwa.[8]

---

7 Marva Dawn, *Kufikira kopanda…* (Grand Rapids: Eerdmans, 1995).

8 Mbali za chigawo ichi zatengedwa kuchokera kwa David Jeremiah. *Kulambira*. (CA: Turning Point Outreach, 1995), 20-24.

Atsogoleri wolambira nthawi zambiri amafunsa, “kodi kulambira kwathu kunatakasa gulu? Kodi unafikira mwa njira yakuti anthu anakondwa? “Malemba amationetsa kuti mafunso ofunikira kwambiri ndi, “kodi kulambira kwathu kunalemekeza Mulungu? Kodi tinalambira Mulungu monga m’mene Iye amafunira? Kodi kulambira kwathu ndi kovomerezeka kwa iye.”

Kulambira Kumene Mulungu Amakana

Mulungu savomera kulambira kosadziwa.

Mzimayi wa ku Samariya sanadziwe chimene amalambira (Yohane 4:22). Ku Atene, Paulo anaona anthu amene anapembedza mulungu osadziwika (Machitidwe 17:23).

Mu phunziro 2 tiphunzira chikhalidwe cha Mulungu amene timamulambira. Ngati sitidziwa Mulungu, kulambira kwathu ndi kosadziwa; ndi kulambira kwa mulungu wosadziwika. Timalondola ndondomeko ya mwambo,[9] koma kulambira kwathu ndi kwa Mulungu osadziwika. Kulambira kuyenera kumaonetsa chikhalidwe cha Mulungu kwa wolambira. Tiziimba nyimbo zimene zimayankhula za chikhalidwe cha Mulungu; tizilalikira uthenga umene umanena za chikhalidwe cha Mulungu. Tisamalore kulambira kwa mulungu osadziwika.

Mulungu savomera kulambira kwa mafano.

Fano ndi china chilichonse chimene chimatenga malo oyenera Mulungu mu dera lililonse la moyo. M’madera a ena a dziko mafano ndi milungu yosema. M’madera ena a dziko, mafano ndi ntchito, mabuku a ku banki, nyumba, komanso chikondwelero. China chlilichonse chimene chimatenga malo a Mulungu pamoyo wathu ndi fano. Ngati timapita ku tchalitchi pasabata koma kulora zinthu zina kukhala ndi ulamuliro omaliza pa miyoyo yathu ya tsiku ndi tsiku, ndiye kuti tikutumikira mafano.

Mulungu savomera kulambira kodzichepsa.

» Perekani zitsanzo za kulambira kodzichepsa.

Mneneri Malaki anachenjeza kuti kulambira kwa Israeli kwakhala kokhumudwitsa kwa Mulungu. Anaukira Mulungu, “Takhumudwitsa Mulungu motani?” Malaki anayankha,

---

9 Ndondomeko ya mwambo ndi chikozero cha nthawi ya kupembedza kwa gulu. Ndondomeko ya mwambo ikhoza kukhala ya dongosolo labwino lokhala ndi ndondomeko zolembedwa. Ikhoza kukhala yofotokozera yopanda malangizo olembedwa kwa wolambira. Muphunziro ili, mawu akuti “ndondomeko ya mwambo” m’manenedwe onse. Kulambira kokozekera kukhoza kukhala kukhala kopanda phindu, kapena ukhoza kudzazidwa ndi kupezeka kwa Mulungu.

> Mukamapereka nsembe nyama zosaona, kodi sicholakwa? Mukamapereka nsembe nyama zachilema kapena zodwala, kodi sicholakwa? Kayeseni kuzipereka kwa bwanamkubwa wanu! Kodi akasangalatsidwa nanu? Kodi akazilandira? Akutero Yehova Wamphamvuzonse (Malaki 1:8).

Sakanapereka nyama yopunduka ngati mphatso kwa wolamulira dziko lawo, koma koma anabweretsa nyama zopunduka ngati nsembe kwa Mulungu wamphavu zonse wa chilengedwe.

Anthu ambiri amakhulupirira kuti maonekedwe a kupembedza kwa kunja siofunikira chifukwa Mulungu amayang'ana mkati. Ndi zoona kuti Mulungu amaona mtima. Komanso, ndizomveka bwino m'malemba monse kuti maonekedwe a kulambira kwa kunja ndi ofunikira kwa Mulungu. Eksodo ndi Levitiko amapereka ndondomeko zomveka bwino za zofuna za Mulungu pa kulambira. Malangizo a mu Chihema anali olondola. Mulungu anapereka malangizo a tsatanetsatane a zovala zovalidwa ndi a nsembe. Pa Eksodo 39-40, liwu lakuti, "monga Yehova analamula Mose" akubwerezedwa maulendo 13 pakufuna kuonetsa kumvera kwa Israeli. Zoona zenezeni za kulambira zinali zofunikira kwa Mulungu. Anafuna zabwino za Israeli.

Timapereka kulambira kochepsa tikamapereka zochepa zathu kwa Mulungu. Ngakhale kuti sitiperekanso nsembe za nyama kwa Mulungu, mfundo izi zikadali zofunikira. Mafunso amene anaperekedwa mu Malaki akupereka maganizo a mafunso amene tiyenera kufunsa za kulambira kwathu Lero.

- **Abusa**: "Kodi mkanakozekera uthenga wanga mosamala ngati nduma ikanakhala kuti ili mgulu? Kodi ndikubweretsa nsembe yolumala kwa Mulungu?"
- **Woimba**: "Kodi ndiyenera kukozekera mosamala ngati oimba otchuka ali mu mgulu? Kodi ndikubweretsa nsembe yolumala kwa Mulungu?"
- **Anthu wamba**: "Kodi ndimvetsera mozama ku uthenga uwu olalikira akanakhala pulezidenti? Kodi ndikubweretsa nsembe yolumala kwa Mulungu?"

Mulungu savomera kulambira kodzikweza.

Mulungu savomera nsembe imene ili yochepera pa ubwino wathu. Koma, pali chiopsezo chimene tiyenera kupewa. Mulungu savomera nsembe ya mtima wonyada ndi odzikweza. Ngakhale timabweretsa zabwino zathu kwa Mulungu, tiyenera kuzindikira kuti palibe chimene timabweretsa ndi choyeneradi kwa Mulungu. Chopereka chathu chachikulu ndi chochepa kwambiri ndi zimene Mulungu amayenera. Timabwera mu kupezeka kwa Mulungu mwa kudzichepetsa, osati ndi mtima wonyada ndi odziyenereza.

Kulambira Kumene Mulungu Amavomereza

Ngati awa ndi machitidwe a kulambira amene ali osavomerezeka kwa Mulungu, kodi ndi kulambira kotani kumene Mulungu amavomera?

Kulambira kovomerezeka kumalunjika kwa Mulungu.

Monga Yesaya 6, Chivumbulutso 4 amayamba ndi zenera la kumwamba. Pa Chivumbulutso 4, chidwi cha wolambira chili pa amene wakhala pampando wachifumu, kulambira koona kumalunjika kwa Mulungu. Kulambira koona kumalozera kwa Mulungu ngati amene ali woyenera kulambira.

Kulambira komvomerezeka kumapereka ulemelero kwa Mulungu umene umamuyenera.

Masalimo 96:7-8 akuwonetsa cholinga cha kulambira:

> Perekani kwa Yehova, inu mabanja a anthu a mitundu ina, perekani kwa Yehova ulemerero ndi mphamvu. Perekani kwa Yehova ulemerero woyenera dzina lake; bweretsani chopereka ndipo mulowe m’mabwalo ake.

Kulambira kumapereka ulemu kwa Mulungu umene umamuyenera. Pakusatengera nyimbo zimene timaimba, maimvaimva amene timatakasa, kapena mayankho amene timalandira kwa owonelera, kulambira kumene sikubweretsa ulemelero kwalephera kukwaniritsa cholinga chake.

Cholinga cha kulambira ndikudzipezera dalitso; cholinga cha kulambira ndi kupereka ulemu ndi ulemelero kwa Mulungu. Pamene tikulambira, tidzadalitsika – Koma dalitso lathu sicholinga cha kulambira. Cholinga cha kulambira ndi kulemekeza Mulungu.

Kuzindikira cholinga cha kulambira kumasintha funso limene timafunsa nthawi zambiri lokhudza kulambira. M’malo mofunsa kuti “Kodi ndinakondwera kulambira kwalero?” tidzafunsa kuti “kodi kulambira kwalero kunalemekeza Mulungu?” Pamene tizindikira bwino za cholinga cha Kulambira, tidzasintha chidwi chathu pa ife kupititsa kwa Mulungu.

Kulambira kovomerezeka ndi kulambira mu mzimu ndi m'choonadi.

Mukukambirana kwa Yesu ndi mzimayi wa ku Samariya pa (Yohane 4:24). Ichi ndi chitsanzo choyenera cha kulambira.

Nthawi zambiri tikamanena za kalambiridwe, timanena za maimbidwe, ndondomeko ya mwambo, ndi machitidwe ena a ndondomeko. Anthu ambiri akhumudwitsidwa chifukwa

cha kusapezeka kwa chidziwitso chozama cha kulambira mu mpingo wa Chipangano Chatsopano:

- **Tikudziwa amaimba masalimo**. Sitidziwa kuti ndi mamvekedwe anji amene amagwirirsa ntchito; sitikudziwa nyimbo zatsopano zimene anaimba**.**
- **Tikudziwa amapemphera**. Sitikudziwa ngati amapemphera mokweza, ngati amapemphera mtimagulu ta anthu ocheoa, kapena wina amatsogolera pemphero. Sitikudziwa ngati amagwiritsa ntchito mapemphero olembedwa (Masalimo) Kapena mapemphero ochokera pakamwa pawo.
- **Tikudziwa kuti amalalikira**. Sitidziwa kuti amalalikira nthawi yaitali bwanji, kuti ndi ndi kalalikidwe kotani kamene amagwiritsa ntchito, kapena mwambo ulionse wa mapemphero unali ndi uthenga.

Kupatula kuchokera mu Chipangano Chatsopano komanso uthenga umene unalembedwa zaka zamakumi ochepa, tili ndi chidziwitso chochepa cha kalambiridwe ka mpingo woyambirira.[10]

Kwa ophunzira, kusoweka kwa chidziwitso uku ndikokhumudwitsa. Komabe, mwina izi zikuonetsa kuti zinthu zimene timazitenga kukhala zofunikira kwambiri sizimene Mulungu amazitenga kukhala zofunikira kwambiri! Pamene Yesu ananena za njira ya kulambira, Anakhazikika pa zinthu ziwiri: mzimu ndi choonadi. Zinthu ziwiri izi ndi zofunikira kwambiri ku kulambira koona.

Kulambira mu mzimu ndi kutheka kukutanthauza mzimu wa munthu. Kulambira kusamakhale mwambo osaikirako nzeru; pamakhala mzimu. Kulambira uku kumene kuli kweikweni; kumachokera mumtima.

KULAMBIRA MU MZIMU?

Mu 1994, Mpingo wa Vineyard ku Toronto unanena za chitsitsimutso pamene anthu anaseka, kubangula ngati mikango, ndi “kubzikula” (kusanza-ngati kubzikula kuti achotse maimvaimva). Mu nthawi ya “kuseka koyera,” anthu nthawi zina anapita ku zina. M’malo mwa kukulora Mawu a Mulungu kuti agwire ntchito mozama m’miyoyo ya ofunafuna, “Dalitso la Toronto” linafuna

10 Chiphunzitso cha *Didache* ndi uthenga wa ufupi kuyambira kumapeto zaka za zaka oyambirira ndi kumayambiliro kwa zaka za mazana awiri *Didache* mumakhala chiphunzitso cha makhalidwe a Chikhristu, miyambo ya mpingo, ndi kayendetsedwe ka mpingo.

kuthana ndi maimvaimva. Kodi uku ndi kulambira mu Mzimu? Kodi ndi kulambira kwenikweni?

Kulambira mu choonadi kumagwirizana ndi chiphunzitso cha baibulo. Ndizoposa kumva bwino kapena maimvaimva. Ngati abusa ndi atsogoleri a kulambira, timaunikanso mbali iliyonse ya kulambira kwathu, pakufunsa kuti "kodi uku ndi kulambira koona?" Mawu amene timalalikira, mawu amene timaimba, ndi mawu amene timapemphera azikhala okhulupirika ku malemba. Mulungu sakondwera ndi mawu opanda kanthu; iye akufuna kulambira mu mzimu ndi choonadi (Yohane 4:24).

KULAMBIRA MU CHOONADI?

Abusa a Bill akudziwa za kufunikira kwa nyimbo. Amayamikira nyimbo zakale, komanso amalandira nyimbo zatsopano. Nyimbo imene yakhala yotchuka m'mipingo yambiri imaphunzitsa kuti okhulupirira ambiri amagwa mu uchimo kenaka ndi kufunafuna kubwezeretsedwa. Nyimboyi sipereka lonjezo la chigonjetso cha moyo wa Chikhristu. Kumvetsera nyimbo iyi, Bill anati "nyimbo iyi siyoona ku malemba, koma ndi nyimbo chabe. Anthu amakonda nyimbo; mawu ndi osafunikira." Kodi uku ndi kulambira mu choonadi?

ZOOPSEZA KULAMBIRA: ZOLOWA M'MALO MWA KULAMBIRA KOONA

Yesu anayankhula za kulambira koona. Ngati kuli kulambira koona, ndiye padzakhalanso kulambira kwabodza. Martin Luther nthawi zambiri ananena za mwambi wa ku German, "Kulikonse kumene Mulungu wamanga mpingo, Satana amaika malo ake pafupi." Nthawi zambiri tavomereza kulambira kuti titsatire zofuma za chikhalidwe koma osatsatira zofuna za Mulungu amene timalambira. Kodi zina zolowa m'malo mwa kulambira koona ndi chiyani?

Kulambira kwa Chisangalaro

Kulambira kwa chisangalaro ndi kulambira kumene kumakhazikika pa zofuna zamunthu, osatizokondweretsa Mulungu. Kuli ma McDonald 35,000 dziko lonse lapansi. Ogula okwana 68 million amadya ku McDonald patsiku limodzi. Ichi sichifukwa chakuti a McDonald

amapereka chakudya chabwino. Koma ndi chifukwa chakuti a McDonald amakhala opezekeratu, okhazika komanso amapereka chisangalaro.

A McDonald ndi Wolambira mwa chisangalaro amayesa chipambano ndi manambala. A McDonald amadzikweza "Anthu odutsa 300 million asamalidwa."a McDonald amadzikweza "Tinakula ndi 17% chaka chatha."

Pali zofuna zochepa za Wolambira mwa chisangalaro. Wolambira mwa chisangalaro amapereka nyimbo zabwino, mikuzamawu yosangalatsa, komanso zinthu zopatsa chidwi – pamtengo wochepa. Wolambira mwa chisangalaro amakusa gulu koma nthawi zambiri chakudya cha uzimu pamakhala palibe ndipo salimbikitsa thanzi la uzimu. Ndibwino kufuna kukopa anthu, koma kulambira mwa Chisangalaro sikulambira koona.

Kulambira Kosungira Mbiri ya Chikhalidwe

Zochitika mu kulambira kosunga mbiri ya chikhalidwe ndi kosiyana ndi kulambira mwa chisangalaro. Mosungira mbiri ya chikhalidwe, muli kutsindika kwakukulu kwa kusunga chikhalidwe. Mosungira mbiri ya chikhalidwe mwambiri satsindika za kutengapo mbali kwa munthu komanso kudzipereka. Simuitandidwa kuti muike chojambula chanu pa khoma la za luso losungira mbiri!

Mu kulambira kosunga mbiri ya chikhalidwe, cholinga chathu choyamba ndi chikhalidwe ndi machitidwe ake. Timaimba nyimbo zimene mpingo wakhala ukuimba. Tiimanyadira tokha mu kukhulupirika kwathu ku chikhalidwe. Koma ndizotheka kwa anthu kukhalapo sabata ndi sabata koma osakumana ndi zofuna za Mulungu za kudzipereka kwa munthu. Ndizotheka kupita ku tchalitchi sabata ndi sabata ndi kuona pa ma ulaliki (uthenga, nyimbo, mapemphero) popanda kusinthika kwa moyo. Ndi bwino kulemekeza chikhalidwe chathu. Koma kulambira kosunga mbiri ya chikhalidwe si kulambira koona.

Kulambira kwa Kalasi

Mu kalasi, m'phunzitsi ndiye oyang'anira. M'phunzitsi amasankha zakuti kalasi iphunzire. M'phunzitsi amaphunzitsa; ophunzira amamvetsera ndi kulemba notsi. Kutengapo mbali kumayendetsedwa ndi m'phunzitsi.

Mu kalasi ya kulambira, m'busa ndiye oyang'anira. Uthenga ndiwo chindunji cha mapemphero; chilichonse chimangothandizira. Mpingo ulipo kuti umvetsere ndi kutenga notsi. Kulambira kumachepetsedwa kufika pa maphunziro. Ndi zabwino kufuna kunena choonadi mu kulambira kwathu; tiyenera kufotokozera choonadi kwa wolambira athu, koma kalasi ya kulambira si kulambira.

Kulambira Koona

Kulambira koona kumalunjika kwa Mulungu. Kulambira koona kumafusa, “Kodi Mulungu amafuna chiyani?” Kulambira koona kumandithandiza kudziona ndekha kudzera m’maso a Mulungu — ndipo izi ndi zosautsa kwa munthu amene sakufuna kusinthidwa ndi Mulungu. Kulambira koona kumakhala ndi kuoloka, nsembe, kudzipereka. Kulambira koona kumasintha wolambira.

KUMALIZA: UMBONI WA MARITA

Kodi kulambira ndikofunikira motani? Mverani umboni wa Marita.

“Ndine munthu wogwira ntchito. Munthu amene ayenera kusesa pasi, kuphika chakudya, ndi kusamalira zonse za panyumba. Chimenechi ndicho chilimbiko changa; ndili ndi mphatso yakutumikira.

“Ndimakumbukira tsiku limene Yesu anatichezera kunyumba yanga yaing’ono ku Betaniya. Ndinali ndi mantha kukhala ndi m’phunzitsi ofunikira mu nyumba mwathu. Ndimafuna chilichonse chikhale bwino. Pambuyo pake Luka analemba, Koma Marita anatanganidwa ndi zokonzekera.’ (Luka 10:40). Ndinali otangwanika kuyesetsa kuti zonse zikhale bwino.

“Pamene ndinali wotangwanika kusamalira nyumba Mariya anakhala mu chipinda china kumvetsera Yesu. Sindinali wokondwa; Ndimafunika thandizo! Pambali pake, ndi mzimayi sakufunika kuphunzira kuchokera kwa Rabbi.

Koma Marita anatanganidwa ndi zokonzekera zonse zimene zimayenera kuchitika. Iye anabwera kwa Yesu namufunsa kuti, “Ambuye, kodi simusamala kuti mchemwali wanga wandisiya kuti ndichite ntchito yonse ndekha? Muwuzeni andithandize!” (Luka 10:40). Sindidzaiwala yankho lake. Anandiyang’ana nagwedeza mutu wake. Ambuye anati, “Marita, Marita, ukudandaula ndi kuvutika ndi zinthu zambiri, koma chofunika n’chimodzi chokha. Mariya wasankha chinthu chabwino, ndipo palibe angamulande chimenechi” (Luka 10:41-42).

“Kodi Mbuye amayankhula chiyani kwa ine? Samatanthauza kuti kutumikira sikofunikira. Asanabwere kodzatichezera, Yesu ananena za mwambi wa Msamariya wa chifundo – nkhani yakutumikira (Luka 10:25-37). Yesu samanena kuti kutumikira; Amandiuza kuti **Kutumikira kwanga kuyenera kuzichokera mu kulambira kwanga**. Chinthu chofununikira ndi kulambira. Ambuye anati, “Marita, Marita, ukudandaula ndi kuvutika ndi zinthu zambiri” (Luka 10:41).

“Tsiku limenelo ndinaphunzira phunziro la moyo. Kutumikira kwanga sikunalowenso mmalo mwa kulambira kwanga. Kuyambira tsiku limenelo kupita m’tsogolo, ndinatenga nthawi yokhala ndi Mariya pamapazi a Yesu; ndinatenga nthawi ya kulambira.”

FUFUZANI

Dzifufuzeni nokha, “Kodi ndingakhale wolambira wabwino motani?” onani madera ena amene mungapange kulambira kwanu kukhala kogwirizana kwambiri ndi kufotokozera kulambira kwa baibulo.

KUBWEREZA KUONANSO PHUNZIRO 1

1. Kodi kulambira ndi chiyani?

   - Kulambira ndi kugonjera kolemekeza (Chivumbulutso 4:10-11).
   - Kulambira ndi utumiki (Aroma 12:1).
   - Kulambira ndi kuyamika (Masalimo).
   - Kulambira ndi chiyanjano (Machitidwe 2:42).
   - Kulambira kumakhudza zonse za moyo (Yakobo 1:26-27).

2. Kodi ndi chifukwa chiyani kulambira kuli kofunikira?

   - Mu kulambira timaona Mulungu (Yesaya 6:1-8).
   - Mu kulambira timadziwona tokha ndipo timasinthika (Yesaya 6:1-8).
   - Mu kulambira timaona dziko lathu (Yesaya 6:1-8).
   - Kulephera kulambira kumatilekanitsa ndi Mulungu (Aroma 1:18-25).

3. Zolinga za kulambira:

   - Mu kulambira timakumana ndi Mulungu.
   - Mu kulambira timakoza khalidwe la Chikhristu.
   - Mukulambira, timamanga gulu la Chikhristu.

4. Kodi ndi kulambira kotani kumene kuli kovemerezeka kwa Mulungu?

   - Kulambira kovomerezeka kumalunjika kwa Mulungu (Chivumbulutso 4).
   - Kulambira komvomerezeka kumapereka ulemelero kwa Mulungu umene amayenera (Masalimo 96:7-8).
   - Kulambira kovomerezeka ndi kulambira mu mzimu ndi m'choonadi (Yohane 4:23-24).

NTCHITO YA PHUNZIRO 1

1. Kodi Baibulo limafotokozera kulambira motani? Lembani mayankho odzala tsamba limodzi pa mawu opezeka pa:

   - Masalimo 111:1-2
   - Masalimo 147:1
   - Masalmo 150
   - Yesaya 6:1-8
   - Chivumbulutso 4

   Ngati mukuphunzira pagulu, kambiriranani yankho lanu mu kukumana kwa kalasi yanu yotsatira.

2. Pakuyamba kwa phunziro lotsatira, werengani mafuso a mayeso aphunziro mosamala pakukozekera.

NTCHITO YAPHUNZIRO
MBIRI YA ULENDO WAMASIKU 30 YA KULAMBIRA[11]

Muchita ntchito iyi mu phunziro lonseli. Pamapeto pa phunziro, mupereka ripoti kuti mwamaliza ntchito iyi. Mupereka mbiri ya ntchito yanu kwa mtsogoleri wa kalasi.

Tsiku lili lonse la masiku 30, mukhala ndi mphindi zochepa kulingalira chimodzi mwa chikhalidwe cha Mulungu. Ndi zabwino kuchita ntchito m'mawa kuti muganizire za chikhalidwe mkati mwa tsiku lonse. Kulingalira kumatanthauza kuganizira mozama za china chake.

Pezani kope losalembamo kuti mugwiritse ngati molembamo mbiri. Yambani tsiku lililonse ndi pemphero kufunsa Mulungu kuti adzivumbulutse yekha kwa inu. Kenako, tsegulani buku la Masalimo ndipo yambani kuwerenga. Cholinga cha nchito iyi ndi kulingalira, osati kuwerenga zochuluka. Mukhoza kuwerenga vesi limodzi kapena Salimo lonse.

Pamene mukuwerenga, onani chikhalidwe chimodzi cha Mulungu kapena chifanifani cha Mulungu. Chikhalidwe ndi mbali ya chiganizo cha khalidwe la Mulungu – chifundo chake, chiyero chake, chisamaliro chake. Chifanifani cha Mulungu chimafanizira Mulungu ku chinachake – ndi m'busa, thanthwe, m'thunzi wathu.

Mukapeza chikhalidwe kapena chifanifani chimene chikuyankhula kwa inu, lembani chikhalidwe pamwamba pa tsamba la mbiri yanu ya phunziro. M'musi mwake, lembani vesi limene likugwirizana ndi chikhalidwe chimenecho.

Ganizirani za chikhalidwe komanso chimene chimanena za Mulungu. Mukapemphera, lembani maganizo anu okhudza Mulungu ndi chikhalidwe ichi. Ili sipepala la maphunziro; ndi pepala la mbiri yanu ya kulambira. Tsiku lonse, ganizirani za Mulungu ndi chikhalidwe cha Mulungu. Yamikani Mulungu chifukwa cha chimene ali. Mukachita izi kwa masiku 30, mudzakhala ndi chidziwitso chozama cha Mulungu.

---

11 Ntchito iyi yatengedwa kuchokera mu Louie Giglio, *Mpweya Umene Ndimapuma: Kulambira ngati njira ya Moyo* (Sisters, OR: Multnomah Publishers, 2003).

MAYESO A PHUNZIRO 1

1. Munapatsidwa matanthauzo atatu a kulambira ku mayambiliro a phunziro ili. Lembani tanthauzo limene munaloweza.

2. Lembani maganizo anayi a kulambira.

3. Pamene mayi wa ku Samaria anatsutsa za malo opembedzerapo, yesu anawonetsa _____ opembedzerapo.

4. Mu Masalimo, liwu lakuti _____ limagwiridwa ntchito pa kunena chimwemwe cha kulambira.

5. Molingana ndi Yakobo, kodi kulambira kumene kuli koona komanso kosadetsedwa kumakhala ndi mbali ziwiri zotani?

6. Nenani zifukwa zinayi zimene kulambira kuli kofunikira.

7. Molingana ndi phunziro ili, kodi ndi makhalidwe atatu oti a kulambira amene ali ovomerezeka ndi Mulungu?

8. Lembani Yohane 4:23-24 kuchokera pakuloweza.

PHUNZIRO 2

MULUNGU NDI WOLAMBIRA

ZOLINGA ZA PHUNZIRO

1. Kuzindikira chithunzi cha Mulungu monga mwa Baibulo komanso ntchito yake mu kulambira kwathu.
2. Kudziwa za zofuna za Mulungu kwa wolambira.
3. Funani kudzifaninzira ndi zofuna za Mulungu pa wolambira.
4. Yamikirani chisomo cha Mulungu pakulola munthu kuti alowe mkupezeka kwake pakulambira.

KUKONZEKERA PHUNZIRO ILI

Lowezani Chivumbulutso 5:9-14.

CHIYAMBI

Gulu laling'ono linakhala pansi ndi kuyamba kukambirana za mutu wa phunziro wa Baibulo wa sabata lino. Funso lokambirana linali, "Kodi Mulungu ali ngati ndani ndipo timamulambira motani?"

Sarah anayankhula poyamba. "Ndikamaganiza za Mulungu, ndimaganiza za gogo wamwamuna wa ndevu zoyera komanso zazitali. Amationa ife ngati adzukulu ake, zimamumvetsa chisoni tikamachimwa, koma amatikonda ndi kumvetsetsa kuti tikuyesetsa. Sindikuganiza kuti Mulungu amasamala mmeme ife timalambirira malinga tikamaonetsa kuti timamukonda."

Hannah anayankha, "Ndimaganizira za Mulungu ngati tate wovuta. Sakhala pafupi ndi ana ake, koma amayang'ana kuti awone ngati akumvera. Mu kulambira, timafunika kuonetsa kuti ndife ogonjera ndi omvera. Sindikonda nyimbo zimene zimapanga Mulungu kukhala

ngati bwenzi lathu; tiyenera kudziwa kuti ndi Mbuye wathu wa kumwamba ndife akapolo ake! Ndimapita ku tchalitchi kuti ndikapeze chimene Mulungu amafuna kuti ine ndizichita."

Abigail sanali wokhutira ndi lina lililonse la mayankho awa. "Ndimaganiza za Mulungu ngati bwenzi. Baibulo limati Mulungu amakonda kupereka mphatso zabwino kwa ana ake. Ndimapita kutchalitchi kuti ndi dziwe zimene Mulungu akufuna andichitire. Ndimapemphera ndikumuuza zimene ndikufuna. Ndimamvetsera uthenga ndi nyimbo kuti ndiphunzire m'mene Mulungu adzadalitsile moyo wanga. Mulungu amafuna kundipatsa mphatso zabwino; ndimapita ku tchalichi kuti ndi kalandire mphatso zimenezo."

Onse mwa azimayi awa ali ndi maganizo osiyana okhudza Mulungu. Chifukwa cha chimenecho, mzimayi aliyense ali ndi chiyembekezo chosiyana cha mwambo wakulambira.

Sarah akuyembekezera Mulungu wokhala ngati gogo amene sasamala kwambiri za kulambira kwathu. Mukuganiza kwake kwa kulambira, akuganiza kuti munthu aliyense adzapembebedza mwa njira imene ili yabwino kwa iye. Sarah wayenera kukhala odabwitsidwa ndi kulambira mu Chihema. Kumeneko anayenera kuphunzira kuti Mulungu amakhala okhudzika ndi kulambira kwathu.

Hannah akuona Mulungu ngati wapatali komanso wosasamala. Wayenera kukhala wosowa mtendere ndi chiyankhulo cha pa Masalimo komanso kuona mtima kwa madandaulo a Yobu kwa Mulungu. Mwambo wake wa kulambira udakhala wapatali pakati pa wolambira ndi Mulungu. Pemphero lidzakhala lachizolowezi komanso lokhazikika. Nyimbo zidzakhala zambiri koma zosamukhudza. Hannah sakanakondwera ndi chiyanjano chapafupi chimene chimapezeka mu mipingo imene imasonkhana munyumba ya zaka zoyambilira.

M'maganizo a Abgail, Mulungu ndi otumikira amene alipo kuti akumane ndi zosowa za anthu. Pamene alutuluka mu mkusonkhana, funso lake ndi ili, "Kodi ndinatengapo chiyani?" Nyimbo kwa iye zimamveka bwino. Mapemphero amalunjika pa zosowa za munthu. Uthenga unali wabwino ndipo umayankhula ku zosowa zake. Abgail akanakhala okhumudwa ndi kulambira kwa mu Kachisi. Kulambira kwa mu Kachisi kunali kubweretsa nsembe kwa Mululungu, osati Mulungu kubweretsa mphatso kwa munthu.

Aliyense mwa azimayi awa akuyang'ana mwambo wakulambira umene umagwirizana ndi kuganiza kwake kumene alinako pa Mulungu. Kumvetsetsa kwathu kwa Mulungu kuli ndi zotsatira zazikulu pa kulambira kwathu.

» Kambiranani za kuganiza kwanu kwa Mulungu. Kodi maganizo anu amakhudza kulambira kwanu?

Muphunziro ili tiona mafunso awiri:

1. Kodi ndi ndani amene timamulambira?

Pakuti kulambira ndi kupereka kwa Mulungu ulemu omuyenera, tikamadziwa zochuluka za Mulungu, ndipamene tidzakonzekeretsedwe kwambiri ku kulambira koona. Kuona kolakwika kwa chifanizo cha Mulungu kumalowera ku kulambira kosokonekera.

Chithunzi cha kupembedza fano kumaonetsa fundo iyi. Baala anali mulungu wa chonde, mulungu kuchulukitsa kopanda malire. Kodi aneneri a Baala analambira motani? Mosaleletseka ndi mochuluka. Choncho iwo anafuwula kwambiri ndi kudzichekacheka ndi malupanga ndi mikondo, potsata miyambo yawo, mpaka kutuluka magazi" (1 Mafumu 18:28).

2. Kodi Mulungu amafuna chiyani kwa wolambira ake?

Pakuti Mulungu ndi woyera, kodi timalowa motani mukupezeka kwake? Kodi Mulungu amafuna chiyani kwa iwo amene amamulambira?

Milungu yabodza ngati Baala ndi Moleki sinali yoyera; wolambira awo sanafunike kukhala woyera. Wolambira Baala anakhala ngati Baala, a makhalidwe oipa.

Mulungu owona ndi woyera. Chifukwa cha ichi, amafuna anthu woyera. Wolambira Yehova amakhala ngati Yehova; amafunika kuti akhale anthu woyera wolambira Mulungu woyera.

KODI TIMALAMBIRA NDANI?

Tayelekezani kuti mukunyadira kulowa kwa dzuwa.[12] Nthawi yomweyo mwasiya kuonelera kulowa kwa dzuwa kuti mudzijambule chithunzi: "Ine ndikuonerera kulowa kwa dzuwa" ichi chimatchedwa "chindekha"

**"Mulungu ndinu...
wam'mwambamwamba,
wabwino koposa;
wachifunndo komaso
wolungama koposa;
wobisika kwambiri komanso
wopezeka kwambiri;
wokongola kwambiri komanso
wamphamvu kwambiri;
wogwira ntchito nthawi
zonse, wokhala akupumula
nthawi zonse.
osonkhanitsa, koma
osasowa kanthu;
wochilikiza ndi woteteza;
wolenga komanso wosamarira;
wofunana, koma
wokhala ndi zonse."**

**Zotengedwa kuchokera
kwa Augustine**

12 Zambiri mwa izi zinatengedwa kuchokera kwa Warren Wiersbe, *Kupembedza koona*, (Grand Rapids: Baker Books, 2000), Mutu 5.

kudzijambula wekha. Munthu amene amazijambula chindekha amakhala ndi chidwi ndi kupezeka kwake kusiyana ndi zochitika zimene akuonelera.

Mulungu ndi oyenera kulambira kwathu kwabwino. Koma tikamaona pa mulingo wa kupembedza kwathu osati pa Mulungu amene timamupembedza, ndiye kuti tapanga chindekha cha chipembedzo. ("Ine ndikulambira Mulungu"). Tisamalore zofuna zathu zokometsa kulambira kwathu kuti zichotse chidwi chathu pa Mulungu amene timamupembedza!

C.S. Lewis analemba za kupembedza mafano kopereka chidwi ku mwambo wa kulambira osati kwa Mulungu. Chaposachedwa, D.A. Carson anachenjeza kuti tikhoza kuyesedwa "kulambira *Kulambira* osalambira Mulungu."[13]

Kulambira sikulambira koona kufikira nditadzipereka ndekha mu kulemekeza Mulungu. Mukulambira koona ndimapereka chidwi chambiri kwa Mulungu kusiyana ndi machitidwe a kulambira kwanga.

Monga tinaona muphunziro 1, lamulo loyamba limatiuza wofunika kumulambira, "Ine ndine Yehova Mulungu wako amene ndinakutulutsa ku Igupto, m'dziko la ukapolo. Usakhale ndi milungu ina koma Ine ndekha" (Eksodo 20:2-3). Pakuti kulambira kumatanthauza kupereka kwa Mulungu ulemu umene amayenera, phunziro la kulambira liyenera kuyamba ndi kufunsa kuti Mulungu ndi ndani? Nyimbo zinayi mu buku la Chivumbulutso likupereka yankho lambali imodzi ya funso ili.

Timapembedza Mlengi (Chivumbulutso 4)

» Werengani Chivumbulutso 4 mokweza. Tengani nthawi kupereka masomphenya a zochitika za kumwamba. Kodi chaputala ichi chikutiuza chiyani za Mulungu amene timamupembedza?

Ndi zenera lake lopita kumwamba, Chivumbulutso 4 akutipatsa chithunzithunzi cha Mulungu amene timamupembedza.

Mlengi ndi wa Ulamuliro.

Mulungu amakhala pampando wachifumu pamwamba padziko. Mawu akuti *mpando wachifumu* akugwiritsidwa ntchito maulendo 14 mu chaputala ichi. Ndi Mulungu wamphamvu zonse. Kulambira kuyenera kuzindikira ulamuliro onse wa Mulungu. Mu kulambira, timaonetsa kugonjera kwathu kwa Mulungu wamphamvu zonse. Ndi Tate wokonda, koma wa ulamuliro onse.

13 Kuchokera kwa D.A. Carson, *Kulambira kwa Buku*, (Grand Rapids: Zondervan, 2002), 31.

Mlengi ndi woyera.

M'malemba onse, Mulungu akuoneka kukhala Mulungu woyera.

- Mulungu akuuza a Israeli, "Uza gulu lonse la Aisraeli kuti, 'Khalani oyera mtima chifukwa Ine, Yehova Mulungu wanu, ndine Woyera" (Levitiko 19:2).
- Mulungu akutamandidwa, "Inu ndinu Woyera, wokhala pa mpando waufumu" (Masalimo 22:3).
- Ndipo Aserafiwo amafuwulirana kuti "Woyera, woyera, woyera Yehova Wamphamvuzonse. Dziko lonse lapansi ladzaza ndi ulemerero wake" (Yesaya 6:3).
- Chamoyo chilichonse chinali ndi mapiko asanu ndi limodzi, ndipo chinali ndi maso ponseponse ndi m'kati mwa mapiko momwe. Usana ndi usiku zimanena mosalekeza kuti, "Woyera, woyera, woyera ndi Ambuye Mulungu Wamphamvuzonse, amene munali, amene muli ndi amene mukubwera!" (Chivumbulutso 4:8).

Timalambira Mulungu Woyera.

Mlengi ndi wamuyaya.

Anali alipo ndipo adzakhala (Chivumbulutso 4:8).

Davide ananena za kudabwitsa kwa chilengedwe ngati zenera pa ulemerero wa Mulungu. "Zakumwamba zimalengeza za ulemerero wa Mulungu; thambo limalalikira ntchito za manja ake" (Masalimo 19:1). Chaputala choyamba cha Genesis chikuyamba ndi Mulungu ngati Mlengi; Buku lomalizira lamu Baibulo likutikumbutsaso kuti Mulungu ndi Mlengi komaso adzalamulira mpaka muyaya pa zolengedwa zake.

Kutsindika uku kukuonetsa chindunji choyenera chakulambira. Ife amene tili olengedwa timalambira Mulungu Mlengi. Kulambira mwachidziwikire ndikwa Iye, onsati kwa ife. Pamene tidzipereka tokha mwakulambira kwa Mulungu, kumwamba kumalengezanso ulumerero wake.

Timalambira Muwomboli (Chivumbulutso 5)

» Werengani Chivumbulutso 5 mokweza. Kodi nkhani yonena za ukulu iyi ikutiuza chiyani za Mulungu amene timalambira?

Ngati a Khristu, tisamasiye nzeru zathu za kudabwa tikakumbukira kuti mfumu ya chilengedwe inapereka mawomboledwe athu. Pa Chivumbulutso 5, tikuonelera, pamene mwana wankhosa wa Mulungu, Muwomboli wadziko, akupembedzedwa. Yesu amatchedwa "mwana wankhosa" maulendo 28 mu Buku la Chivumbulutso. Ichi ndi chimodzi mwa zithunzithunzi zazikuluzikulu mu Chivumbulutso.

Timalambira Muwomboli chifukwa cha chimene Iye ali.

Ndi Mkango wa fuko la Yuda. Ndi Muzu wa Davide. Ndi mwana wankhosa amene anaphedwa. Ndi mwana wankhosa amene minyanga isanu ndi iwiri komanso maso asanu ndi awiri (Chivumbulutso 5:6), chizindikiro ungwiro. Mukulambira, timalemekeza Yesu chifukwa cha chimene Iye ali. Kulambira ndi "chikondwelero cha ungwiro wa ulemelero wa Khristu" (John Piper).

Timalambira Muwomboli chifukwa cha kumene Iye ali.

Pa Chivumbulutso 5:6, Yesu ndi thima la kupembedza kwa kumwamba. Ali pakati pa mpando wachifumu ndi zamoyo zinayi komanso akulu. Wolemba wa Aheberi akupereka lonjezo lodabwitsa lakuti nkhoswe yathu yakhala ku dzanja lamanja la mpando wachifumu wa Mulungu (Aheberi 12: 2).

Timalambira Muwomboli chifukwa cha zimene anachita.

Pakufuna kuona kuyenera kwa Mulungu, aphunzitsi ena anapereka maganizo akuti tiyenera kulambira Mulungu pa chifukwa chimene iye ali chokha. Yohane wovumbulutsa akuonetsa kuti kulambira kwa kumwamba kumalemekeza Mwana wankhosa chifukwa cha zimene wachita. Ndipo angelowo anayimba ndi mawu ofuwula akuti, "Mwana Wankhosa amene anaphedwayu ndi woyenera kulandira ulamuliro, chuma, nzeru, mphamvu, ulemu, ulemerero ndi mayamiko" (Chivumbulutso 5:12).

Machitidwe awa akuoneka mu Masalimo. Malalimo 134 amatilamulira kuyamika Yehova. Sapereka chifukwa; timamulambira chifukwa ndi Mulungu. Otsatira ndi Masalimo 135-136, amene amayamika Mulungu chifukwa cha zimene wachita mu mbiri ya Israeli. Chikhalidwe cha Mulungu, komanso ntchito zake zamphamvu, ndizoyenera matamando. Tiyenera kuyamika Mulungu chifukwa cha chimene Iye ali **ndi** ndi zimene wachita.

Timalambira Mfumu (Chivumbulutso 11:15-18)

Chivumbulutso 11 amapereka maganizo ena a kulambira kwa kumwamba. Mu nkhani iyi, akuluakulu amalambira mfumu imene yakhala pampando woyenera. Ngakhale kuti ma ufumu a dziko amamuukira iye, ayenera kugonjera ku ulamuliro wake. Mngelo wachisanu ndi chiwiri anawomba lipenga lake, ndipo kumwamba kunamveka mawu ofuwula amene anati, "Ufumu wa dziko lapansi uli m'manja mwa Ambuye athu ndi Khristu wake uja, ndipo adzalamulira mpaka muyaya" (Chivumbulutso 11:15).

Mu nyimbo iyi, mfumu ikutamandidwa chifukwa cha kuweruza kwake kolungama padziko. Nyimbo iyi ikutikumbutsa kuti Mulungu amalamulira mwa ukulu. Ngakhale mafuko anali okwiya, koma Mulungu anaweruza molungama.

Kulambira ndi kulambira mu choonadi. Kulambira koona sikuchepetsa chiweruzo chodabwitsa cha Mulungu. Komanso, kulambira kwa Chivumbulutso ndi kofanana ndi kulambira kwa Masalimo. Masalimo 96 ndi nyimbo yatsopano ya kwa Yehova. Mu nyimbo imeneyi, Mulungu akutamandidwa pakati pa a mitundu. Akuopedwa kuposa milungu yonse. Akuopedwa chifukwa adzaweruza anthu molungama. Kulambira koona kumadziwa kuti tiyenera kuopa Mulungu; timamulambira ngati mfumu.

Timalambira mkwati Wopambana (Chivumbulutso 19:1-9)

Mu kalasi ya kafukufuku wa Baibulo, m'phunzitsi anafunsa, "Kodi ndi chifukwa chiyani simukonda Chivumbulutso?" ophunzira m'modzi anayankha, "Ndi ochititsa mantha!"

Chifukwa chimene ophunzira awa amapeza Chivumbulutso kukhala ochititsa mantha ndi chakuti amadumpha zigawo zabwino za buku. Amakhazikika pa chiweruzo chimene chimabwera kwa owukira Mulungu. Umenewo ndiwo uthenga ofunikira mu Chivumbulutso. Koma kwa a Khristu, uthenga ofunikira kwambiri ndi chigonjetso cha Mulungu wathu!

Chivumbulutso 19 amafotokozera uthenga uwu. Chaputalachi chili ndi kufotokonzera kwa nyanja ya moto imene imayaka ndi sufire (Chivumbulutso 19:20) ndi mbalame zimene zimadya mnofu wa mafumu, wa akulu a nkhondo wa anthu a mphamvu… (Chivumbulutso 19:18) Uku ndiko kuopsa kwa iwo amene amaukira mfumu. Kwa iwo amene amalambira mfumu mwa kugonjera kolemekeza, Chivumbulutso 19 ndi nyimbo ya kukondwera. Mkazi wachiwerewere amene anaononga dziko ndi dama lake (Chivumbulutso 19:2) waonongedwa. Mkwati wagonjetsa adani ake ndikulandira mkwatibwi wake woyera ku madyelero a ukwati wa mwana wankhosa (Chivumbulutso 19:9).

Pakulandira chigonjetso chachikulu ichi, Kenaka ndinamva "chimene chinamveka ngati gulu lalikulu, ngati mkokomo wamadzi othamanga ndipo ngati kugunda kwakukulu kwa bingu, ndipo anati, 'Haleluya! Pakuti Ambuye Mulungu wathu Wamphamvuzonse akulamulira. Tiyeni tisangalale ndi kukondwera ndi kumutamanda! Pakuti nthawi ya ukwati wa Mwana Wankhosa yafika, ndipo Mkwatibwi wakonzekeratu'" (Chivumbulutso 19:6-7).

Mu Kulambira, timayamikira mkwati wogonjetsa. Kulambira kwathu kumaonetsera za tsogolo kuti Yesu aKukonzekera mkwatibwi. Chifukwa china chimene kulambira kuli kofunikira ndi chakuti kulambira kumatilimbikitsa kukhala moyo wa Chikhristu wa chipambano mu dziko la mavuto. Mu Kulambira timakumbukira kuti, "Koma ife ndife nzika za kumwamba ndipo tikudikirira mwachidwi Mpulumutsi wochokera kumeneko, Ambuye Yesu Khristu. Iyeyo, ndi mphamvu imene imamuthandiza kukhazikitsa zinthu zonse pansi pa ulamuliro wake, adzasintha matupi athu achabewa kuti akhale ofanana ndi thupi lake la ulemerero" (Afilipi 3:20-21).

Nyimbo zinayi izi zimatipatsa zochokera mu Chivumbulutso zimatipatsa masomphenya a Mulungu amene timalambira. Mu kulambira, sitidziona ife eni koma pa Mulungu.

Mukulambira, timagwada pamaso pa Mlengi, mu kulambira, timayamikira Muwomboli; mu kulambira timakondwerera Khristu amene ali mfumu; mukulambira, timayembekezera umuyaya pamaso mkwati wogonjetsa.

Uyu ndi Mulungu amene timamulambira. Izi zimatifikitsa pa fuso, "Kodi ndi ndani amene angalambire? Kodi Mulungu amafuna chiyani kwa iwo amene amabwera mkupezeka kwake?"

KODI MULUNGU AMAFUNA CHIYANI KWA WOLAMBIRA?

Mu kukambirana kwake ndi mzimayi wa ku Samariya,[14] Yesu ananena chiganizo chokumbukirika. Atamuuza kuti wolambira woona adzalambira Atate, mu mzimu ndi choonadi, Yesu anati Atate akufuna anthu otero kuti amulambire (Yohane 4:23). Mulungu akufuna mtundu wapadera wa wolambira, iye amene amalambira mu mzimu ndi choonadi. Mulungu amafuna wolambira.

Kodi ndi makhalidwe otani amene Mulungu amafuna mwa iwo amene amalambira iye? Aliyese akhoza kupezeka pa mwambo wa kulambira, aliyense akhoza kuimba nyimbo za matamando; aliyense akhoza kunena mapemphero. Komabe Mulungu wapereka malangizo a padera a makhalidwe a wolambira owona. Malo amodzi owonapo izi ndi Masalimo 15.

» Werengani Masalimo 15. Kodi akutiuza chiyani za moyo wa wolambira?

Masalimo 15 ndi salimo la pemphero. Likufotokozera kukambirana kwa wa nsembe ndi wolambira pakhomo la Kachisi. Wolambira amafuna polowera mu Kachisi woyera wa Mulungu. Pakuyankha fuso la wolambira "Kodi ndi ndani angalowe?" Wansembe akufuna khomo la polowera. Machitidwe omwewa akugwititsidwa ntchito pa Masalimo 24:3-6 ndi Mika 6:6-8. Masalimo 15 amagawidwa patatu:

1. Funso: Kodi ndi ndani amene angalambire?
2. Yankho: Kufotokozera wolambira
3. Kumaliza kauniuni: Lonjezo kwa wolambira

Funso la: Kodi ndi ndani amene angalambire? (Masalimo 15:1)

Polowera pa Kachisi wolambira akufunsa, "YEHOVA, ndani angathe kukhala m'malo anu opatulika? Ndani angathe kukhala m'phiri lanu loyera?" Mayankho awa akupereka zoyenereza zitatu za wolambira.

---

14 Zambiri za izi zatengedwa kuchokera mu "Mafikidwe a Wolambira kwa Mulungu" lolembedwa ndi Ronald E. Manahan, zikupezeka mu Chaputala 2 cha *AKupembedza Koona*, Lokonzedwa ndi Herbert Bateman. (Grand Rapids: Kregel Books, 2002).

Wolambira amadziwa mantha a umulungu.

Salimo ili likuonetsa kuti kulowa mu kupezeka kwa Mulungu sikwachizolowezi. Wolambira owona amadziwa kuti Mulungu ndi woyera ndipo kuti ndife osiyanitsidwa ndi Iye.

M'malemba monse, muli mamvekedwe a mantha ophatikizana ndi Mulungu. Pa Phiri la Sinai, anthu anachenjezedwa kukhala kutali ndi phiri kumene Mulungu anayankhula ndi Mose (Eksodo 19:7-25). Pa phiri la Kusandulika, ophunzira anali ndi mantha kwambiri (Mateyu 17:6).

Kwa okhulupirira, mantha a umulungu sichiopsezo chimene chimachotsa munthu pa kupezeka kwa Mulungu. M'malo mwake, ndi ulemu umene umapangitsa munthu kuti afikire kwa Mulungu ndi kudzichepetsa. Wolambira sayenera kuyenda mukupezeka kwa Mulungu osakonzekera.

Wolambira owona amalambira modzichepetsa.

Wolambira anafunsa "Ndani angathe kukhala m'malo anu opatulika?" Alendo ogonera ndi nzika zochokera dziko lina. Ndi alendo, amene alibe ufulu umene nzika zilinawo...

Masalimo 15 amafuna kuti wolambira azindikire kuti ndife alendo mu kupezeka kwa Mulungu. Pakuti Mulungu ndi woyera, sitiyenera kukhala pamenenepo. Palibe kanthu kuti udindo wathu ndi otani pamoyo, koma tiyenera kulowa mkupezeka kwa Mulungu ndi maganizo odzichepetsa. Ndife alendo ake.

Wolambira owona amakondwerera chisomo cha Mulungu.

Chifukwa chakuti timazindikira chiyero cha Mulungu, timakondwerera chisomo cha cha Mulungu akatilandira mu nyumba yake. Wolambira amene anafunsa, "M'ndani angathe kukhala m'phiri lanu loyera"? anafunsa funso ili molimba mtima kuti akhoza kuitanidwa mu nyumba ya Mulungu. Mulungu anakhazikitsa ubale ndi Israeli; Kukulambira kwa Chiyuda anakondwerera ubale wapamwambawu.

Masalimo 103 ndi kuitanira kukulambira "Lemekeza Yehova, moyo wanga." Masalimo 103 ali ndi chikumbutso cha chisomo chimene chimatilola kulowa mkupezeka kwa Mulungu.[15]

"Monga bambo amachitira chifundo ana ake, choncho Yehova ali ndi chifundo ndi iwo amene amamuopa; 14pakuti Iye amadziwa momwe tinawumbidwira, amakumbukira kuti ndife fumbi" (Masalimo 103:13-14). Mulungu amene anatilenga kuchokera ku fumbi watiitana mwachisomo kukulambira! Tikamalowa mkulambira, timakumbukira chisomo cha Mulungu. Ndi chisomo chimene chimalora fumbi kulowa mkupezeka kwa Mulungu Mlengi wa zonse.

---

15 Kuona uku kukuchokera kwa Richard Averbeck, "Kulambira Mulungu mu Mzimu."

Kulambira kowona kumakhala ndi mantha a umulungu, kudzichepetsa, komanso chisomo. Wolambira a Chiyuda analemekeza Kachisi chifukwa inali nyumba ya Mulungu Woyera.[16] Anakozekera mosamala kulambira pofuna kuonetsa kudzichepetsa koyenera pamaso pa Mulungu. Anakondweranso mkulambira. Kulambira kwa Chiyuda kunali kodzala ndi mayimbidwe, zida, zonunkhirisa zamtengo wapatali, komanso mamvekedwe amene anakondwerera kupezeka kwa Mulungu kwa anthu ake.

Lero lino, tiyenera kulowa mu nyumba ya Mulungu ndi mantha a umulungu. Tiyenera kuzindikira kusayenera kwathu pamaso pa Mulungu. Koma kulambira kwathu kuyeneranso kukondwerera chisomo cha Mulungu chimene chimatilandira mu mkupezeka kwake. Pemphero lakale la chiyanjano limati, "Tikubwera osati chifukwa kuti ndife oyera, koma chifukwa chakuti taitanidwa." Uku ndi kulambira kumene kumakondwerera chisomo cha Mulungu.

Yankho la: Kufotokozera Wolambira (Masalimo 15:2-5)

Pakuyankha funso la "Kodi ndani angalowe mu nyumba ya Mulungu?" wansembe anapereka kufotokozera kwa wolambira. Wolambira amayenda wosalakwa pamaso pa Mulungu. Amakhala osamala ndi zochitira ena. Amakana iwo amene amakana Mulungu, koma amalemekeza amene amaopa Mulungu. Munthu amene amalambira Mulungu mowona adzakhala ngati Mulungu.

Yankho ili likutikumbutsa kuti kulambira kumakhudza madera onse a moyo wathu. Kulowa mkupezeka kwa Mulungu kumafunika kumvera konse kwa thunthu. Davide sanayembekezere munthu onena kuti "Ndine mwana wa Mulungu, koma sindikhala ogonjera ku lamulo la Mulungu." Kulowa mu mkupezeka kwa Mulungu kumafunika kugonjera ku ulamuliro wa Mulungu.

Wolambira owona amakhala moyo wa umulungu.

Masalimo 15:2 akupereka kufotokozera kwa wolambira. Iwo amene amalowa mkupezeka kwa Mulungu ayenera kuyenda wopanda chilema; izi zikunena za moyo wa ungwiro m'madera onse. Ayenera kuchita zimene zili zabwino nthawi zonse. Ayenera kuyankhula choonadi chamkati (Kapena chochokera) mumtima. Mawu awa akufotokozera moyo wokhazikika wa wolambira. Zonse za moyo ndizokhudzidwa ndi kulambira.

16 Pofika nthawi ya Yesu, ulemu uwu unali utatha ndipo polowera pa Kachisi panasanduka malo a msika. Yesu anathanangitsa osintha ndalama amene anaononga kachisi, kumusandutsa "phanga la a chifwamba" (Mateyu 21:12-13).

Wolambira woona amakhala ndi ubale wabwino ndi anthu.

Monga ngati m'mene Davide sakanaganizira za munthu amene anati "Ndine mwana wa Mulungu koma sinditsatira lamulo la Mulungu, sindikhala ndi ondizungulira moyenera."

Munthu amene amalowa mkupezeka kwa Mulungu ayenera kukhala munthu amene amakhala ndi ubale wabwino ndi anthu. Iye:

- Sachita miseche ndi lilime lake.
- Sachita choipa kwa mzake.
- Sachita chipongwe mzake; sajeda.
- Amatsutsa amene amakana Mulungu.
- Amalemekeza amene amalemekeza Mulungu.
- Amakhaka owona ku Mawu ake.
- Sapereka ngongole za chiongoladzanja chosayenera kwa osauka.
- Sachita zolakwa zolakwa kwa osalakwa pakulandira ziphuphu.

Munthu amene amalowa m'kachisi wa Mulungu ndi munthu wolungama, mkati ndi kunja komwe. Wolambira woona ndi munthu wa ungwiro Wolambira woona salola miyambo ya kulambira kutenga malo a moyo wa tsiku ndi tsiku wa kumvera.

Kumaliza kauniuni: Lonjezo kwa wolambira (Masalino 15:5)

Masalimo 15 akumaliza ndi lonjezo kwa wolambira; "Amene amakongoletsa ndalama zake popanda chiwongoladzanja ndipo salandira chiphuphu pofuna kutsutsa anthu osalakwa. Iye amene amachita zinthu zimenezi sadzagwedezeka konse" (Masalmo 15:5). Munthu amene amakhala omvera malamulo a Mulungu amalonjezedwa chitetezo cha Mulungu. Masalimo 15 amasiyana ndi Masalimo 1 ndi mafotokozeredwe a umulungu ndi lonjezo lake la dalitso la Mulungu pa munthu wa umulungu.

Masalimo 15 amawonetsa chimene Iye amafuna kwa iwo amene amamulambira. Masalimo ayenera kuwerengedwa ngati lamulo (izi ndi zimene Mulungu amafuna") komanso ngati lonjezo. ("Izi ndi zimene Mulungu adzachita kwa iwo amene adzapempha kwa Iye) Pakuona Yesaya 6, tikuzindikira kuti ndi Mulungu amene amapereka mphamvu kwa wolambira kuti akhale omvera; ndi Mulungu amene amayeretsa milomo yodetsedwa; ndi Mulungu amachita malamulo a pa Masalimo 15 kuti atheke. Kulambira koona kumadalira pa chisomo cha Mulungu. Zimatheka osati mwa kuyesetsa kofooka, koma mwa chisomo cha Mulungu mwa kulambira; Atate amafuna kulambira Iye. Osaiwala chisomo cha Mulungu.

FUFUZANI

Dzifunseni nokha, "Kodi ndili ndi mtima ndi manja a wolambira owona?" Werengani Masalimo 15 ngati mayeso. Pambuyo pa mawu alionse funsani "Kodi izi zikufotokoza ine? Kodi ndine okonzeka kulambira?"

Werenganinso Masalimo 15, ngati pemphero la panokha. "Yehova' mundipatse mphamvu kuti ndiyende opanda chilema ndikuchita chimene chili chabwino… Mundipatse chisomo kuti ndipewe miseche ndi oneneza." Malizani pa kumva lonjezo la Mulungu, "Iye amene amachita zinthu zimenezi sadzagwedezeka konse."

ZOOPSEZA KULAMBIRA: CHINYENGO

Yesu anayankhula za anthu amene anadzitenga okha kukhala a katswiri a kulambira. Alembi ndi Afarisi anali osamalitsa kutsatira ndondomeko iliyonse ya kulambira, malamulo a Baibulo komanso miyambo ya Chiyuda. Anali ofulumira kuweruza aliyense amene analephera kutsatira ndondomeko iliyonse ya miyambo yawo. Koma, Yesu anaweruza kulambira kwawo chifukwa anali a chinyengo.

Afarisi anadandaula kuti ophunzira a Yesu sanatsatire mwambo wa chipembedzo wosambitsa manja awo. Inu anthu achiphamaso, Yesaya ananenera za inu kuti, "'Anthu awa amandilemekeza Ine ndi milomo yawo, koma mitima yawo ili kutali ndi Ine. Amandilambira Ine kwachabe ndi kuphunzitsa malamulo ndi malangizo a anthu'" (Mateyu 15:7-9). Afarisi, monga ngati wolambira abodza a nthawi ya Yesaya, anatchedwa wolambira wonama ndi Yesu chifukwa cha zolephera ziwiri:

1. "'Anthu awa amandilemekeza ine ndi milomo yawo, koma mitima yawo ili kutali ndi ine'" (Mateyu 15:8).
2. "'Amandilandira ine kwachabe ndi kuphunzitsa malamulo ndi malangizo a anthu'"(Mateyu 15:9).

Tiyenera kukhala wosamala pofuna kupewa kuopsa kolambira mwa chinyengo. Kulambira kwathu kuyenera kuzichokera mkati, ndipo kulambira kwathu kuzitsogozedwa ndi Mulungu, osati malangizo a anthu amene adzikweza kufikira pofanana ndi Mawu a Mulungu.

KUMALIZA: UMBONI WA WOLAMBIRA

Tikawerenga Masalimo 15 osakumbukira ntchito ya chisomo pa moyo wa Chikhristu, tikhoza kupeza mfundo yabodza yakuti tiyenera kugwirira ntchito kuti tipeze mwayi wa kulambira. Koma, Masalimo 15 akuonetsa chimene Mulungu amatichitira, osati zimene timachita, kuti tilandiridwe mu nyumba yake.

Kodi ndi ndani amene amalandiridwa ku kulambira? Mverani maumboni ena odabwitsa a wolambira. Amaonetsa kuti kulambira sikukhala woyenera; kulambira ndi kubwera modzichepetsa mkupezeka kwa Mulungu ndi kusinthika ndi chisomo chake.

Mfarisi akuyankhula:

Ndikudziwa kuti mukhoza kumvetsa chifukwa chimene ndinakhumudwira ndi chiphunzitso cha Yesu. Ndine munthu wabwino. Sindiswa malamulo. Ndimasala ndi kupereka chakhumi. Ngati pali munthu wina oyenera kukondera kwa Mulungu, anayenera kukhala ine! Ndimapita ku nyumba kuonetsa kuti ndine munthu wabwino. Koma chifukwa chiyani Mulungu angakane kulambira kwanga?

Munthu wamba akuyankhula:

“Kunena moona mtima ndine wodabwa ngati mfarisi! Sindinali otsimikizika kuti ndikhoza kulowa mu Kachisi. Ndinali kutali kwambiri ndi anthu abwino. Ndimaganiza kuti palibe amene angandione. Ndinafuna chifundo cha Mulungu ngakhale kuti sindiyenera chifundo. Chondidabwitsa ndinapita kunyumba wolungamitsidwa. Moyo wanga unasinthika mu kulambira.”

Munthu wachuma akuyankhula:

“Ndimapereka ndalama zochuluka ku Kachisi. Ndikuganiza kuti Yesu anayenera kuti asunthike ndi chopereka changa. Ndikaponya chopereka mu mtanga wa chopereka, aliyense amadziwa kuti ‘Bambo Ndalama’ ali pano. Ndikuganiza kuti Mulungu amadziwa m’mene ndimaperekera!”

Mzimayi wosauka wamasiye akuyankhula:

“Ndinali ndi manyazi kuponya chopereka changa mu mtanga wa chopereka. Ndinali ndi ndalama za chitsulo zing’onozing’ono ziwiri. Aliyense amapereka zochuluka.; ine pafupifupi ndinalibe kanthu. Koma kulambira ndi kupereka chimene chili chabwino kwa Mulungu. Ndinaganiza kuti palibe amene angazindikire kachopereka kanga kakang’ono, koma wina wake anatero. Yesu anaona chimene ndinapereka! Ndipo Iye anati ndinapereka kuposa aliyense. Sindikudziwa kuti Yesu amatanthauza chiyani ndi mawu amenewu, koma ndine wokondwa ndinapereka chabwino!”

KUKAMBIRANA KWA GULU

» Kuti phunziro ili limveke bwino, Kambiranani izi:

Yohane wakhala M'khristu kwa zaka zambiri. Amadziwa kuti kupezeka ku tchalitchi, kuwerenga Baibulo, ndi pemphero ndi zofunikira, koma ndizovuta kwa Iye kumva kupezeka kwa Mulungu mu zochitika izi. Zimaoneka zopanda kanthu kuposa mwambo chabe. Kodi mungamuthandize motani Yohane kuona Mulungu mu Kulambira?

KUBWEREZA KUONANSO PHUNZIRO 2

1. Kuzindikira kwathu kwa Mulungu ndi kofunikira pa kulambira chifukwa chithunzi chosokonekera cha Mulungu chidzabweretsa kupembedza kosokonekera.

2. Kulambira kuyenera kulunjika kwa Mulungu, osati machitidwe abwino a malambiridwe athu.

3. Chivumbulutso amapereka chithunzi cha Kulambira kwa kumwamba:

   - Kulambira kwa kumwamba ndi Kulambira kwa Mlengi amene ali wa mphamvu zonse, woyera, wamuyaya.
   - Kulambira kwa kumwamba ndi kulambira kwa Muwomboli.
   - Kulambira kwa Kumwamba ndi kulambira kwa kwa Mfumu.
   - Kulambira kwa Kumwamba ndi kulambira kwa mkwati Wogonjetsa.

4. Salimo 15 ndi Salimo limene limafotokozera zofuna za Mulungu kwa wolambira. Wolambira owona.

   - Kudziwa mantha a umulungu.
   - Kulambira mu kudzichepetsa.
   - Kukondwerera chisomo cha Mulungu.
   - Kukhala miyoyo ya umulungu.
   - Kukhala mu ubale wabwino ndi anthu.
   - Kulandira lonjezo la Mulungu la chitetezo komanso ndi dalitso.

NTCHITO YA PHUNZIRO 2

1. Masalimo 120-134 ndi kusonkhanitsa pamodzi kwa nyimbo za a ulendo opita ku Yerusalemu. Werengani Masalimo awa pamene mukuyankha mafunso ali m'musimu.

SALIMO	MAFUNSO OFUNIKA KUYANKHA
120	Kodi malo a Meseke ndi Kedera ali kuti? Kodi ndi chifukwa chiyani kulambira mu Yerusalemu kuli kofunikira kwa mulendo amene amakhala mu Meseke kapena Kedara?
122	Kodi Salimo ili tikutiphunzitsa chiyani za maganizo athu pa kulambira?
123	Kodi vesi 2 likutiphunzitsa chiyani za ubale wa wolambira ndi Mulungu?
124	Kodi mukuphunzira chiyani za kulambira mu nyengo zowawa kuchokera mu Salimo ili?
126	Kodi kulambira kumagwirizana motani ndi pakati pa mitundu? Onani vesi 2.
130	Kodi Salimo ili likutiphunzitsa chiyani za kufunikira kwa kuvomereza mu kulambira?
131	Kodi wolemba Masalimo akudzikonzekeretsa motani ku kulambira? Kodi ndi njira ziti zodziwika zimene mungatsate kuti mutsatire chitsanzo ichi?
133	Masalimo 133, Yohane 17:20-23, ndi Aefeso 4:1-16 onse amayankhula za umodzi ndipo amanena za moyo wa mpingo mwanjira ina. Kodi umodzi umayenderana motani ndi kulambira mu umoyo wa mpingo?
134	Kodi Masalimo 134 ndi mathero oyenerea motani pa zolemba za masalimo wolambira?

2. Koyambirira kwa phunziro lotsatira, mudzalemba mayeso ochokera pa phunziro ili. Werengani mafunso a mayeso mosamala pa Kukonzekera.

MAYESO A PHUNZIRO 2

1. Fotokozani zinthu zitatu zimene timaphunzira za Mulungu Mlengi mu nyimbo ya pa Chivumbulutso 4.

2. Tchulani zifukwa zitatu za kulambira Muwomboli mu Chivumbulutso 5.

3. Kodi uthenga oyambirira wa Chivumbulutso kwa a Khristu ndi uti?

4. Masalimo 15 ndi Salimo la pemphero logawidwa pa magulu atatu.

5. Kodi maganizo a wolambira amene amazindikira kuti ndi mulendo mkupezeka kwa Mulungu ndi otani?

6. Kodi ndi makhalidwe ati awiri ofunikira a wolambira owona kuchokera pa Masalimo 15:2-5?

7. Kodi ndi chifukwa chiyani Yesu anawatcha Afarisi kuti ndi achinyengo?

8. Lembani Chivumbulutso 5:9-14 kuchokera pakuloweza.

PHUNZIRO 3

KULAMBIRA MU CHIPANGANO CHAKALE

ZOLINGA ZA PHUNZIRO

1. Kuyamika chisomo cha Mulungu chimene chimapangitsa Kulambira kutheka.
2. Kulowa mu Kulambira ndi mtima wa kumvera.
3. Kudziwa ntchito ya mwambo mu Kulambira.
4. Kuchita mayamiko ngati gawo limodzi lapakati mu kulambira.
5. Kuzindikira kufunikira koyankhula Mawu a Mulungu mu Kulambira.
6. Kupewa kuopsa kwa kusalinganizika mu kulambira.

KUKONZEKERA PHUNZIRO ILI

Lowezani Mika 6:6-8.

CHIYAMBI

Gulu la Abusa limakumana mwezi ulionse kukambirana zochitika m'mipingo mwawo. Posachedwapa anakambirana za kulambira. Pali kusiyana kwakukulu pakati pa abusa awa pa mutu wa kulambira. Ngakhale kuti ali ndi zikhulupiriro zofanana, akusiyana kwambiri pamachitidwe a kalambiridwe.

James ndi m'busa wa mpingo umene umatsatira za kulambira kwa chikhalidwe cha mtundu. Enock amatumikira mpingo waukulu umene umagwiritsa ntchito njira zambiri zamakono pa kulambira. Gideon akuyesetsabe kuti apeze mtundu wa kulambira umene uli ogwirizana ndi

mpingo wake. Abusa awa akhala akukambirana za kulambira kwa nthawi yaitali koma ndi okhumudwa pakuyesa kwawo kofuna kugwirizana za ndondomeko zosavuta za kulambira.

Lero, Jason akuti, "Mwina takhala tikuona pa cholakwika ichi. Timafunsa, 'Kodi ndi kulambira kwanji kumene timakondwera nako?' mwina tiyenera tifunse kuti, 'Kodi Mulungu amafuna kuti tizilambira motani?' Kodi ndi kulambira kotani kumene *Iye* amakondwera nako? Ngati Mulungu akadati akonze kulambira, kodi kukadaoneka motani?' Ngati titaphunzira m'mene kulambira kwa Baibulo kumaonekera, chimenecho chikhoza kutipatsa chitsanzo chathu cha kulambira lero."

» Ngati Mulungu akadati akonze kulambira, kodi kukadaoneka motani? Fotokozani mwachidule zimene mukudziwa kale za kulambira kwa baibulo.

CHIYAMBI: MULUNGU ANAFUNA KULAMBIRA KOYENERA

Mu Phunziro 2, tinaona kuchokera mu Chivumbulutso kuti kulambira koona ndi kulambira kwa Mulungu owona. Mu Phunziro 3, timafunsa, "Kodi wolambira amamufikira motani Mulungu woyera?"

Anthu ena amati Mulungu sasamala m'mene ife timalambirira; amasamala kuti mtima ulibwino. Ndi zoona kuti mtima uli pachimake pa kulambira. Motero, tili ndi umboni waukulu wochokera m'malemba kuti Mulungu amasamala m'mene akulambiridwira.

Machitidwe a m'mene kulambira kukuchitikira ndi ofunika chifukwa **Kulambira kwathu kumakhudza kumvetsetsa kwathu kwa Mulungu**. Muphunziro limene lapita, tinaona kulambira kosokonekera kuononga chithunzithunzi chathu cha Mulungu. Pamene Israeli analambira Yehova mu njira imene Akanani analambira Mulungu wawo, nthawi yomweyo anakhulupirira kuti chikhalidwe cha Mulungu ndi chophimbidwa komanso osadalilika, monga ngati milungu ya Kanani.[17]

Machitidwe a m'mene kulambira kukuchitikira ndi ofunika chifukwa **m'mene timalambirira ndi kumaonetsera chifukwa chimene timalambira**. Mtima wa chikondi umakondwera ndi kubweretsa kulambira kumene kumalemekeza Mulungu; mtima wodandaula umafuna kulambira mwa njira yanga osati mwa njira ya Mulungu.

Makoleji ambiri ali ndi zoyenereza zina za mapepala a kafukufuku. Amafuna tsamba la pamwamba, mawu a m'munsi ndi malire a pepala. Zinthu izi sizinthu zofunikira kwambiri za papepala; koma zimene zalembedwa ndi zimene zili zofunikira. Komabe aphunzitsi ambiri awona kuti ophunzira amene ali wosamala ndi ndondomeko ndi amene alinso osamala ndi zimene zalembedwa mkati. M'mene pepala lachitikira limaonetsera zimene zili mkati mwa pepala. M'mene ife timalambirira zimaonetsera maganizo a mtima wathu. M'mene

17 IPa Mika 6:6-7, atsogoleri a chipembedzo akuyesa kuchita chiphuphu kwa Mulungu ndi nsembe ya ana. Akuganiza kuti Yehova amayembekezera kupereka nsembe ya mwana imene Moleki analamula.

ife timalambirira nthawi zambiri zimagwirizana ndi chifukwa chathu cha kulambira. Chifukwa cha ichi, Mulungu amasamala m'mene timalambirira.

- Kaini anabweretsa nsembe kwa Yehova. Kaini anali wogwira ntchito panthaka. Anabweretsa zipatso za nthaka, koma Mulungu sanakondwere ndi Kaini komanso nsembe yake. Kukanika kulambira kwa Kaini kunaonetsa malingaliro a mtima wake. Nsembe ya Kaini inali yabwino kwa iye, koma Mulungu sanalole kulambira kwake (Genesis 4:1-5).

- Aaroni anawumba mwana wa ng'ombe wa golide kuti agwiritse ntchito polambira Yehova. Anthu ataona kuti Mose akuchedwa kutsika m'phiri, anasonkhana kwa Aaroni ndipo anati, "Bwera utipangire milungu imene izititsogolera. Kunena za Mose amene anatitulutsa m'dziko la Igupto, sitikudziwa chimene chamuchitikira." Aaroni anawayankha kuti, "Vulani ndolo zagolide zimene avala akazi anu, ana anu aamuna ndi aakazi ndipo muzibweretse kwa ine." Kotero anthu onse anavula ndolo zagolide ndi kubwera nazo kwa Aaroni. Choncho Aaroni analandira golideyo ndipo anamuwumba ndi chikombole ndi kupanga fano la mwana wang'ombe. Kenaka anthu aja anati, "Inu Aisraeli, nayu mulungu wanu amene anakutulutsani m'dziko la Igupto." Aaroni ataona izi, anamanga guwa lansembe patsogolo pa mwana wang'ombeyo ndipo analengeza kuti, "Mawa kudzakhala chikondwerero cha Yehova" (Eksodo32:1-5). Mwina Aaroni anadzitsimikizira yekha kuti akhoza kulambira Mulungu mwanjira imene inasagalatsa anthu, koma Mulungu sanalandire kulambira kwake.

- Nadabu ndi Abihu anaona Mulungu wa Israeli paphiri la Sinai (Eksodo 24:1-11). Anakhala chifupi ndi Mulungu kuposa wina aliyense kupatula Mose, koma patsiku loyamba la usembe wawo mu Chihema, anapereka moto wosaloledwa kwa Yehova. Zotsatira zake, moto wochokera kwa Yehova unawaononga. Mose anafotokozera kwa atate wawo wolira Ana a Aaroni, Nadabu ndi Abihu, aliyense anatenga chofukizira lubani chake nayikamo makala a moto ndi kuthiramo lubani. Iwo anapereka pamaso pa Yehova moto wachilendo, moto umene Yehova sanawalamule. Choncho moto unatuluka pamaso pa Yehova ndi kuwapsereza, ndipo anafa pamaso pa Yehova. Pamenepo Mose anawuza Aaroni kuti, "Pajatu Yehova ananena kuti, " 'Kwa iwo amene amandiyandikira ndidzaonetsa ulemerero wanga; pamaso pa anthu onse

"Mukanakhala wansembe wa Chipangano Chakale, ndipo munatumikira Mulungu ngati m'mene mukumutumikira tsopano, kodi zikatenga nthawi yaitali motani Yehova asanakupheni?"

Warren Wiersbe

(Kuganinzira za kufunikira kwa kulambira)

ndidzalemekezedwa.' " Aaroni anakhala chete wosayankhula. Mose anayitana Misaeli ndi Elizafani, ana a Uzieli, abambo ang'ono a Aaroni, ndipo anawawuza kuti, "Bwerani kuno mudzachotse abale anuwa pa malo wopatulika ndi kuwatulutsira kunja kwa msasa." Choncho anabwera atavala minjiro yawo ndipo anawatenga ndi kuwatulutsa kunja kwa msasawo monga momwe Mose analamulira. Ndipo Mose anawuza Aaroni ndi ana ake Eliezara ndi Itamara kuti, "Musalileke tsitsi lanu nyankhalala ndipo musang'ambe zovala zanu kuti mungafe, ndi mkwiyo wa Yehova ungagwere anthu onsewa. Koma abale anu okha, kutanthauza fuko lonse la Israeli ndiwo ayenera kulira omwalira aja amene Yehova wawapsereza ndi moto. Musatuluke kunja kwa tenti ya msonkhano, mungafe, chifukwa munadzozedwa ndi mafuta a Yehova kukhala ansembe." Choncho iwo anachita monga Mose ananenera (Levitiko 10:1-7). Ansembe awa anapereka nsembe mwanjira yawo m'malo motsatira malamulo a Mulungu. Mulungu sanalole kulambira kwawo.

- Uziya anali mfumu yaikulu. Anachita chimene chinali choyenera pamaso pa Mulungu. 2 Mbiri akufotokonzera kulamulira kwake: "Anthu onse a ku Yuda anakondwera pa kulumbirako chifukwa analumbira ndi mtima wawo wonse. Iwo anafunafuna Mulungu mwachidwi, ndipo anamupeza Iye. Kotero Yehova anawapatsa mpumulo mbali zonse" (2 Mbiri 26:15). Zachisoni, awa simathero a nkhani ya Uziya. "Mfumu Asa anachotsanso Maka agogo ake pa udindo wa amayi a mfumu chifukwa anapanga fano lonyansa la Asera. Asa anagwetsa fanolo, naliswa ndipo kenaka anakaliwotcha ku chigwa cha Kidroni" (2 Mbiri 26:16). Anayesa kulambira Mulungu mwa njira yake ndipo anakanthidwa ndi khate (2 Mbiri 26:1-21). Mulungu sanavomereze nsembe yake.

- Ayuda ochokera ku ukapolo anabweretsa nsembe zachilema ku Kachisi. Kulephera kwawo kubweretsa nsembe zoyenera kunaonetsa khalidwe losasamala la mtima wawo. Sanakonde Mulungu moona, mwakuti Mulungu sanavomere kulambira kwawo (Malaki 1:6-14).

Mulungu amasamalira *m'mene* amalambiridwira. Zitsanzo izi zikuonetsa kuti, kukhala patokha, sitingafikire kwa Mulungu mu njira imene ili yolemekeza Iye. Zimene zimaoneka zoyenera kwa ife zikhoza kukhala zosaloledwa kwa Mulungu. Tiyenera kukhala ndi chitsogozo chake cha kulambira kwathu.

Pakuti kulambira kumatanthauza kupereka ulemu kwa Mulungu, kulambira kuyenera kukhala kokhazikika ndi chikhalidwe cha Mulungu osati zofuna zathu. Sitingathe kutsimikiza patokha zimene zili zokondweretsa kwa Mulungu; tiyenera kuona pa Mawu a Mulungu; tiyenera kuona pa Mawu a Mulungu kuti tiphunzire kulambira mwanjira imene ili yokondweretsa Mulungu.

KUYENDA NDI MULUNGU: KULAMBIRA NGATI UBALEWA CHISOMO

Chithunzi cha Baibulo choyamba cha kulambira chili mu munda wa Eden, “Kenaka munthu uja ndi mkazi wake anamva mtswatswa wa Yehova Mulungu akuyendayenda m’mundamo madzulo a tsikulo, ndipo iwo anabisala pamaso pa Yehova Mulungu pakati pa mitengo ya m’mundamo” (Genesis 3:8). Izi zikuonetsa kufunikira kwa kulambira: chiyanjano chosaonongeka cha pakati pa munthu ndi Mlengi wake. Asanagwe, chiyanjano pakati pa munthu ndi Mulungu sichinali chobisika ndi chimo. Kulambira m’munda wa Edeni kunali kusovuta komanso kosasokonekera.

M’munda, tikuona kuti Mulungu amafuna chiyanjano ndi zolengedwa zake. Kufikira pakugwa, munthu anali kokondwera ndi chiyanjano chathunthu ndi Mulungu; ndikufikira pamene chimo linaononga chikhalidwe cha munthu ndipo munthu anadzibisa yekha kwa Mulungu.

Mu Chipangano Chakale, liwu lakuti *anayenda ndi Mulungu* likugwiritsidwa ntchito kuonetsa kuti kulambira kumakhala ndi ubale ndi Mulungu (Genesis 5:24, Genesis 6:9, Genesis 17:1). Chilichose mwa zitsanzo izi chikuonetsa munthu amene anapanga ubale pakukhala ndi nthawi ndi Mulungu. Kulambira kwabwino kumachokera pa ubale wabwino ndi Mulungu.

Genesis 3:8 akuonetsa kuti kulambira kumachokera pa ubale. Akuonetsanso kuti kulambira kumatheka ndi chisomo cha Mulungu chokha basi. Milungu ya mafano imayembekezera munthu kuti apeze njira yabwino yakuti asangalatse milungu. Mosiyana, Yehova mwachisomo anapereka njira yoyenera ya kulambira. Zitsanzo zitatu zikuonetsa ichi.

Mulungu Anapangitsa Kulambira Kukhala Kotheka kwa Adamu ndi Hava

Pambuyo pakugwa, Mulungu sanafunikenso kufunafuna kapena kulandira kulambira kochokera kwa Adamu ndi Hava. Anaswa lamulo la Mulungu; anaononga chilengedwe chake; sanayenerenso china chilichonse koma chiweruzo.

Atachimwa, Adamu ndi Hava anabisala kukupezeka kwa Mulungu (Genesis 3:8). Panalibe chochita china chilichonse kwa Adamu ndi Hava; sakanayembekezera china chilichonse koma imfa. Chochita chokhacho chimene anadziwa ndi kuthawa wopereka lamulo, koma mu chisomo YEHOVA Mulungu anaitana Adamu. Kulambira kumatheka ndi chisomo cha Mulungu. Kusiidwa patokha, tilibe njira yofikira Mulungu woyera. Ndikudzera mu chisomo chake chokha kuti taitanidwa ku kulambira.

Mulungu Anapangitsa Kulambira Kukhala Kotheka kwa Abrahamu

» Werengani Genesis 18:1-8.

Mu Phunziro 1, tinaona kuti limodzi mwa mawu a Chiheberi la Kulambira ndi (*Shachah*) kutanthauza "kugonjera." Liwu ili likugwiritsidwa ntchito koyamba mu Genesis 18:2. Yehova ndi angelo awiri anaonekera pamene Abramu anakhala pakhomo pa hema wake. Abramu anathamanga kuchoka pakhomo pa hema wake kukakumana nawo ndipo anaweramira pansi. Abrahamu anaweramira pansi – analambira.

Dziwani kuti Mulungu anatengapo mbali mu nkhani iyi; anabwera kudzakumana ndi Abrahamu. Mulungu anapangitsa kulambira kukhala kotheka. Mu Chipangano Chakale monganso mu Chipangano Chatsopano, kulambira kumakhala kotheka mwa chisomo chokha. Nsembe za Chipangano Chakale sinjira zosangalatsira Mulungu wokwiya amene safuna ubale; anapangidwa ndi Mulungu mwini ngati njira ya kubwezereza pakati pa Mulungu ndi munthu wochimwa. Ngakhale kulambira kwa Chipangano Chakale, kulambira kukupangidwa kukhala kotheka mwa chisomo cha Mulungu chokha. Mwa ife tokha, tilibe kuthekera kolambira bwino.

Mulungu Anapangitsa Kulambira Kukhala Kotheka kwa Yakobo

» Werengani Genesis 28:10-22. Kodi nkhani imeneyi ikuwulula chiyani za udindo wa Mulungu pakulambira?

Chimodzi mwa chithunzi chodabwitsa cha kulambira chikupezeka pa Genesis 28:10-22. Palibe china chilichonse mumbiri ya Yakobo chimene chikuonetsa zoyenera wolambira. Sakufikira pa zoyenereza za pa Masalimo 15. Sakufunafuna Mulungu; koma, akuthawa mavuto amene anathawa ndi machitidwe ake omwe a chinyengo. Palibe buku lonena za kulambira limene limati "Kulambira kovomerezeka kumachokera kwa achinyengo amene akuthawa kuzotsatira za machimo awo."

Komabe, Mulungu anadziulula yekha kwa Yakobo ngakhale kuti Yakobo anali wosayenera. Chisomo cha Mulungu chimapangitsa kulambira kutheka ngakhale kwa anthu ena osayenera ngati Yakobo. Warren Wiersbe analemba, "Mulungu amatipatsa mwachisomo pamene tili ndi chiyembekezo chochepa – kapena ngakhale kuyenera. **Kulambira kukasiya kukhala kupezeka kwa chisomo, kumasiya kukhala kupezeka kwa ulemerero**."[18]

Ndikudzera mu chisomo chokha kuti Mulungu amatiitana mu kupezeka kwake. Kulambira kwathu ndi kuvomera kwathu ku chisomo chake. Palibe chimene timachita mu kulambira chimene chili choyenera Iye; ndi chisomo chake chokha chimene chimatilimbikitsa kulambira.

---

18 Warren W. Wiersbe, *Real Worship*, (Grand Rapids: Baker Books, 2000), 72.

Nkhani ya Yakobo imaonetsa chimodzi mwa kusiyana kwakukulu pakati pa kulambira Yehova ndi kulambira milungu yabodza. Wolambira milungu yabodza amamanga maguwa kuti apeze kukonderedwa kwa mulungu wawo. Paphiri la Kalimeli, aneneri a Baala "Choncho iwo anatenga ng'ombe yayimunayo imene anawapatsa, nayikonza. Kenaka anayitana dzina la Baala kuyambira mmawa mpaka masana. Iwo anafuwula kuti, "Inu Baala, tiyankheni ife." Koma panalibe yankho; palibe amene anayankha. Ndipo anavinavina mozungulira guwa lansembe limene anapanga" (1 Mfumu 18:26).

Mu Kulambira kwabodza, munthu amamanga guwa kuti apeze kukondera kwa fano (ntchito).

Mu kulambira, munthu amamanga guwa kuti akondwere kukondera kwa Mulungu (chisomo).

» Werengani 1 Mafumu 18:20-39 kuti muone kusiyana kwa kulambira kwenikweni ndi kulambira kwabodza.

Aneneri a Baala anayesetsa kuitana Baala kuti adzionetse yekha kwa iwo. Machitidwe awa akuoneka obwerezabwereza mu kulambira kwa mafano. Maguwa ndi nsembe ndi kuyesa kufuna kupeza chisomo kuchokera kwa mafano.

Mosiyana, Mulungu mwachisomo akudzionetsa yekha kwa anthu ake mu kulambira. Eliya anamanga guwa lake mostimikizika kwathunthu kuti Mulungu amene anamutumikira ayankha pemphero lake.

> Pa nthawi yopereka nsembe, mneneri Eliya anasendera pafupi ndi guwa lansembe, napemphera kuti, "Inu Yehova, Mulungu wa Abrahamu, Isake ndi Yakobo, lero zidziwike kuti ndinu Mulungu mu Israeli ndipo kuti ine ndine mtumiki wanu, kuti ine ndachita zonsezi chifukwa mwalamula ndinu (1 Mafumu 18:36).

Mu Genesis, makolo anamanga maguwa osati kuti apeze chidwi cha Mulungu koma ngati chikumbutso cha malo amene Mulungu anadziulula yekha. Guwa silinapeze chisomo cha Mulungu; koma chinakondwerera chisomo cha Mulungu. Yakobo akutionetsa kuti kulambira kumatipangitsa ife kukhala woyenera chisomo cha Mulungu; timalambira chifukwa cha chisomo.

Kodi chimachitika ndi chiyani Mulungu akapangitsa kuti kulambira kutheke? Yakobo anasinthika. Zinali zaka 30 kusinthika kwake Kusanamalizike, koma kusinthika kunayamba pa Beteli. Kulambira (ngakhale kulambira kosayenera kwa munthu wosayenera ngati Yakobo) kumatisintha ndipo kumatichitira zimene sitikanatha kuzichitira tokha.

FUFUZANI

Dzifunseni nokha, “Kodi ndasinthika ndi kulambira, kapena palibe chimene ndikuchita? Kodi ndi liti limene ndinasintha zochita zanga, zikhulupiriro, kapena maganizo komaliza chifukwa cha kukumana ndi Mulungu mu kulambira?”

ABRAHAMU: KULAMBIRA KUMAFUNIKA KUMVERA

» Werengani Genesis 22:1-19. Kodi zoyenereza kulambira ndi chiyani mu nkhani iyi?

Abrahamu kupereka nsembe mwana wake kunali kuchita kwakukulu kwa kulambira. Mu nkhani iyi onani kutsindika kwa kumvera kwa Abrahamu. Mulungu anati, “Tenga mwana wako…pita…ukapereke nsembe…” Malamulo atatu. Abrahamu “anatenga mwana wake Isake… Ananyamuka ndikupita… ndikutenga mpeni kuti acheke mwana wake.” Abrahamu akumvera lamulo lililonse.

Nsembe ya Abrahamu yopereka ikuonetsa kuti kulambira koona kumafunika kumvera kwathunthu. Kulambira kumaposa kumva chabe kapena maimvaimva; kulambira kumaposa kumvetsera oimba kapena mlaliki; kulambira ndikuvomera kwa machitachita kwa Mulungu.

Pitaninso ku nkhani ya Abrahamu pa Genesis 18. Koyambira kwa nkhani, tikuona kulambira ngati kumvera. Abrahamu akuona alendo atatu akuyandikira hema wake. Anaweramira pansi. Analambira.

Kenaka tikuona Abrahamu akutumikira motangwanika. Anapereka madzi kuti asambe mapazi awo; anathamangira ku hema kukauza Sara kuti aphike makeke; anakonza chakudya ndikuwaikira. Anatenga udindo wa otumikira wodikilira, anayima pansi pamtengo pamene iwo amadya.

Kufunikira kwa kumvera mu kulambira kukuoneka mu Chipangano Chakale. Nsembe ya Abele inalandiridwa chifukwa inakumana ndi zoyenereza za Mulungu zoperekera nsembe. Abele anatenga ana a nkhosa oyamba kubadwa ndi mafuta nakazipereka kwa Yehova ngati nsembe (Genesis 4:4). Abele mwakumvera anabweretsa zabwino zake. Mosiyana, Kaini anafuna kukwaniritsa ntchito yake mwanjira yosavuta.

Kufunikira kwa kumvera mu kulambira kukuonekera m’moyo wa Sauli. Pamene Sauli sanamvere malamulo a Mulungu kuti awononenge nyama zonse za Amaleki, anazilandira

yekha pakunena kuti nyama zathanzi zasungidwa chifukwa cha nsembe. Koma Samueli anayankha kuti, “Kodi Yehova amakondwera ndi nsembe zopsereza ndi nsembe zina kapena kumvera mawu a ake? Taona, kumvera ndi kwabwino kuposa nsembe, ndipo kutchera khutu ndi kwabwino kuposa kupereka mafuta a nkhosa” (1 Samueli 15:22).

» Werengani 1 Samueli 15:1-23.

Mulungu sadzalola kulambira kuchokera mumtima wopanduka.

Kulambira koona kumailmbikitsa ubale ozama ndi Mulungu. Onaninso nkhani ya Abrahamu. Genesis 18 amayamba ndi utumiki wa Abrahamu kwa Mulungu; chaputala chikuthera ndi ubale. Yehova anafunsa, “Kodi ndimubisire Abrahamu chimene ndikuti ndichite posachedwapa…?” atamva za cholinga cha Mulungu, Abrahamu molimba mtima anakambirana ndi Mulungu pa zoopsa za Sodomu. Kodi ndi chiyani chimene chinachitika? Mtumiki wa Mulungu ndi bwenzinso la Mulungu.

Ndikudzera mu kulambira pamene timadziwa Mulungu moona. Ndi mukulambira pamene timaphunzira mtima wa Mulungu kufikira pakuti tikhoza kufika pofunsa molimba mtima. Kulambira kovomerezeka kumakhala ndi kumvera (utumiki) ndi ubale. Abrahamu wolambira ndi mtumiki wa Mulungu komanso bwenzi la Mulungu.

KULAMBIRA KWA BAIBULO LERO

Kodi mudayamba mwadabwa chifukwa chimene anthu ena amalowa mumapemphero ndipo amafika kukupezeka kwa Mulungu pamene ena amapezeka pamapemphero omwewo koma osaona china chilichonse cha Mulungu? Ena amapereka mu chopereka ndipo amadalitsika; ena amapereka koma osakondwera. Kusiyana kwake ndi mtima womvera.

Palibe kanthu kuti kulambira kwathu ndi kwabwino motani, palibe kanthu kuti olambira ndi aluso motani, palibe kanthu kuti uthenga ndi wamphamvu motani, ngati kulambira sikuchokera mumtima wakumvera, ndikulambira kwa Kaini. Kulambira kwa Kaini kumati, “Ndikhoza kubweretsa nsembe yanga mwanjira yanga. Ndiyabwino.” Kulambira koona kumachokera mumtima wakumvera.

FUFUZANI

Dzifunseni nokha, “Kodi ndine wolambira womvera? Kodi kulambira kwanga kumachokera mu mtima wa Abele kapena mtima wa Kaini?”

NSEMBE: KULAMBIRA NGATI MWAMBO

Kugwa kusanachitike, kulambira kumaoneka mu ubale osavuta pakati pa Mulungu ndi munthu. Chimo lisanaononge chikhalidwe cha munthu, munthu anafunikira ndondomeko yobwerera kukupezeka kwa Mulungu. Mwachisomo, Mulungu anapereka ndondomeko ya nsembe. Nsembe zinakhazikitsidwa ndi Mulungu m'munda pamene anapha nyama ndikugwiritsa chikopa chake kuti apange zovala za Adamu ndi Hava. Levitiko anachita dongosolo la ndondomeko mwa kaperekedwe ka nsembe ya kulambira kwa Israeli (Levitiko 1-7 ndi 16).

Tikamawerenga Eksodo ndi Levitiko, zimakhala zomveka bwino kuti ndondomeko za kulambira ndi zofunikira kwa Mulungu. Kwa iwo amene amati "Mulungu sasamala m'mene timapembedzera malinga tikulambira," Eksodo ndi Levitiko akuonetsa kuti m'mene timalambirira ndikofunikira kwa Mulungu! Mulungu anapereka malangizo okhazikika a m'mene kulambira kulili. Izi, monga vumbulutso kwa Adamu ndi Hava atagwa kale, ndi chizindikiro cha chisomo cha Mulungu. Yehova anapereka malangizo omveka bwino, "Umu ndi m'mene muyenera kufikira Ine." Awa anali machitidwe a chisomo.

Kwa Israeli, kulambira kumayambira asanalowe m'nyumba ya Mulungu. Ndondomeko yokonzekera kulambira inawonetsera kulemekeza kwawo kwa Mulungu komanso nyumba yake. Nyimbo zotamanda zikuonetsa kuti ngakhale ulendo wa ku Yerusalemu unali kulambira (Masalimo 120-134). Miyambo ya kulambira siinali yopanda kanthu; ganizo lililonse la kulambira limakumbutsa wolambira za kufunikira kwa kulambira koona.

Nsembe Zinaimira Kugonjera Kwathunthu kwa Mulungu

Akhristu ena sanamvetse ndondomeko za kaperekedwe ka nsembe ka Chipangano Chakale. Anayelekezera ndondomeko imene Israeli mwadala anaphwanya lamulo la Mulungu, anabwezeretsa nsembe zopanda tanthaunzo, ndipo kenaka nthawi yomweyo anabwereranso ku machimo omwewo ndi mtima wosalapa.

Ndizoona kuti izi zinachitika mu nyengo zina. Pakuyankha, Mulungu anati, "Ndimadana nawo masiku anu achikondwerero ndipo ndimawanyoza; sindikondwera nayo misonkhano yanu. Ngakhale mupereke nsembe zopsereza ndi nsembe zachakudya, Ine sindidzazilandira. Ngakhale mupereke nsembe zabwino zachiyanjano, Ine sindidzaziyang'ana n'komwe" (Amos 5:21-22).

Koma, uku kunali kulephera kwa munthu, osati kwa Mulungu. Ndondomeko ya nsembe inalephera pamene munthu analephera kupereka zimene Mulungu analamula. Chikonzero cha Mulungu chinali nsembe zimene zinaonetsera kulapa kwa mtima koona.

Miyambo imene inaphatikizana ndi zikondwerero inaonetsa Israeli za kufunikira kwa zochitika za kulambira. Ndondomeko iliyonse inanena za kulemekeza Yehova kwa Israeli.

Kulambira kwa Israeli siunali mwambo wopanda kanthu; miyambo iyi inaonetsera zenizeni za kudzipereka ndi kumvera kwawo. Pakusanjika manja pa mitu ya nyama, wolambira amadzifanizira yekha ndi nsembe ya imfa. Pakutero, anali kuvomereza, "Munthuyo asanjike dzanja lake pa mutu pa nsembe yopserezayo, ndipo idzalandiridwa kuti ikhale yopepesera machimo ake" (Onani Levitiko 1:4).

Mulungu Analemekeza Kulambira Koona ndi Kupezeka Kwake

Kulambira kwa Israeli kunapitirira kukonzedwa ndi kumanga kwa Kachisi. Monga zinali ndi kulambira kwa mu Hema, ndondomeko iliyonse ya Kachisi inaonetsera ulemu wa Israeli kumvera Mulungu (2 Mbiri 1-7). Mwambo wa nsembe komanso chizolowezi cha Kulambira kwa mukachisi kunakumbutsa Israeli za kukula kwa Yehova ndi kudzichepetsa kumene ayenera kufikiridwa nako.

Kukonzekera mosamalitsa kwa miyambo ya kulambira kwa mukachisi sikunatchinge kupezeka kwa Mulungu. Umodzi wa mwambo okonzekereka bwino mu mbiri ukhoza kukhala mwambo wa kupereka Kachisi. Davide anakonzekera Kachisi zaka za m'mbuyo. Kachisi atamalizika, Solomoni anatsogorera kupereka Kachisi mumwambo wokongola wofotokozeredwa pa 2 Mbiri 5. Oyimba anayimba azeze ndi zitoliro. Ansembe 120 analiza malipenga. Gulu la kwaya linayimba nyimbo za matamando. Pamene anaimba, "Oyimba malipenga ndi oyimba nyimbo aja amayimba mogwirizana, monga liwu la munthu mmodzi, kutamanda ndi kuyamika Yehova. Mogwirizana ndi malipenga, ziwaya zamalipenga ndi zida zina, anakweza mawu awo motamanda Yehova poyimba kuti, Yehova ndi wabwino; chikondi chake chikhala mpaka muyaya. Ndipo Nyumba ya Mulungu wa Yehova inadzaza ndi mtambo, choncho ansembe sanathe kugwira ntchito yawo chifukwa cha mtambowo, pakuti ulemerero wa Yehova unadzaza Nyumba ya Mulungu" (2 Mbiri 5:13-14).

KULAMBIRA KWA BAIBULO LERO

Anthu ena amatsutsa ndondomeko kapena m'chitidwe wina ulionse wa kulambira. Amakhulupirira kuti mwambo ulionse okonzedwa umaononga kulambira kokhudza mtima. Komabe, kulambira kwa Baibulo kunali kwa ndondomeko!

Ngati titsimikizika kumvetsa Mulungu mwa kulambira, kumulambira kwake kuyenera kucitidwa mosamalitsa. Timakonzekera mwambo osati kufuna kuti ena akhutire ndi kukongola kwa mwambo wathu, koma kubweretsa kwa Mulungu chopereka chathu chabwino cha nsembe ya kulambira.

Mu Baibulo, kulambira kokonzekera mosamala (monga kupereka kwa Kachisi) ndi kukonzekera kulambira kwa ndondomeko yochepa (monga kukumama kwa ma tchalitchi a m'nyumba mu zaka zana zoyambilira) kumadalitsika ndi kupezeka kwa Mulungu. Ndipo kulambira kokonzekera mwa ndondomeko yabwino (monga kulambira kwa mu Kachisi mu nthawi ya Yeremiya) ndi kukonzekera kulambira kwa ndondomeko yochepa (monga

kulambira kwa chisokonezo kwa Akorinto) kumachitika popanda kupezeka kwa Mulungu. Nkhani sikukula kwa ndondomeko; nkhani ndi kumvera komanso njala ya kupezeka kwa Mulungu.

FUFUZANI

Dzifunseni, "Kodi kulambira kwanga kwa pagulu (Kokhazikika kapena kosakhazikika) kumachokera pansi pamtima wakumvera?"

MASALMO: KULAMBIRA NGATI MATAMANDO

Buku la Masalimo linali buku la matamando la Israeli. Linali buku la nyimbo; linali kusonkhanitsa kwa mapemphero; linali chitsogozo kukulambira koona; linali buku la kukhala kolungama. Buku la Masalimo linali thima la kulambira kwa Israeli.

Matamando mu Kulambira

Buku la Masalimo limaonetsa kuti kulambira koona kumakhala ndi kutsindika kwakukulu pa kutamanda. Ndi chiyembekezo cha Masalimo 88, Salimo llililonse limakhala ndi chiganizo cha matamando. Miyambo ya Levitiko ikutikumbtsa za mwambo wa kulambira kwa Baibulo; Masalimo akutikumbutsa za chimwemwe cha kulambira kwa Baibulo. Masalimo 120-134 akuonetsa chimwemwe cha a paulendo a Chiyuda pamene amapita ku Yerusalemu kukalambira. Matamando ndi thima la kulambira.

> **"Khalani otsimikizika pa kukhazikika pa chimwemwe cha mwa Mulungu."**
>
> **Richard Baxter**

Kulambira kopezeka mu buku la Masalimo kukuonetsera chimwemwe cha kulambira koona. Kulambira koona kumakhala ndi chikondwerero cha Mulungu ndi ntchito zake.

Kulira mu Kulambira

Masalimo a kulira akuonetsa chiganizo cha kulambira kwa Baibulo; kulambira kumalola kuti pakhale kuona mtima kwathunthu pakati pa wolambira ndi Mulungu. Mu Masalimo a kulira, wolemba Masalimo akuwonetsera kukhumudwa pa kusoweka chilungamo cha dziko lino.

Pa Masalimo 10:1, wolemba Masalimo anafunsa. "N'CHIFUKWA CHIYANI YEHOVA mwaima patali? Mukudzibisa nokha panthawi ya mavuto?" Kodi ndi chifukwa chiyani Mulungu amalola ochita zoipa kuti achite moukira ndi monyada? Chifukwa chakuti kulambira kumachokera pa ubale ndi Mulungu. Wolambira akhoza kuyankhula ndi kuona mtima komanso kumasuka.

Masalimo 10 amamaliza ndi kulengeza kwa chikhulupiriro mwa Mulungu.

> Yehova ndi Mfumu kwamuyaya; mitundu ya anthu idzawonongeka kuchoka m'dziko lake. Mumamva Inu Yehova, zokhumba za osautsidwa; mumawalimbikitsa ndipo mumamva kulira kwawo. Kuteteza ana amasiye ndi oponderezedwa, ndi cholinga chakuti munthu amene ali wa dziko lapansi asaopsenso (Masalimo 10:16-18).

Kulengeza uku kumatengera pa kukhulupirira mwa Mulungu. Ngakhale ochita zoipa amapitiriza kuchita zoipa, wolemba Masalimo akuyankhula molimba mtima kuti Mulungu adzachita chimene chili cholungama.

Timaona kuona mtima komweku mu buku la Yobu. Kuona mtima kotere kumachokera pa ubale wapafupi komanso wabwino ndi Mulungu. Uku ndi kulambira koona, kulambira kumene kuli kovomerezeka kwa Mulungu.

KULAMBIRA KWA BAIBULO LERO

Kulambira kwa Mulungu kumakhala ndi mitundu iwiri ya matamando; Masalimo ena amanena zifukwa za kulambira; Masalimo ena amalamulira kutamanda koma osanena chifukwa. Kuyamika chifukwa cha chikhalidwe komanso ntchito zamphamvu za Mulungu kumatchedwa "kutamanda kofotokoza"; kulambira kumene kulibe chindunji kumatchedwa "kutamanda kolengeza" Zitsanzo za kutamanda kolengeza ndi Masaliomo 19, Masalimo 105, ndi Masalimo 136. Zitsanzo za kulambira kolengeza ndi Masalimo 148-150.

Mu kulambira kwa lero, mitundu iwiri iyi ya atamando imaimiliridwa ndi makolasi (kutamanda kolengeza) ndi nyimbo (kutamnda kofotokozera). Zonse ziyenera kukhala mbali za kulambira. Kuzama kwa nyimbo kumaphunzitsa choonadi chokhazikika cha chikhalidwe cha Mulungu.

Kutamanda Kolengeza

Oho, kuti malilime zikwizi ayimbe
Matamando a Muwomboli wanga,
Ulemerero wa Mulungu wanga ndi mfumu,
Kupambana kwa chisomo chake![19]

Kulambira Kofotokozera

Linga la mphamvu ndi Mulungu wathu, chitetezo cholimba;
Mthandizi wathu, mu nthawi ya msautso:
Pakuti mdani wathu amafuna kutipatsa tsoka;
Koma ntchito zake ndi mphamvu zake ndi zazikulu, ndi odzadza ndi kudana ndi choipa,
Dziko lonse ndi losafanana naye.[20]

FUFUZANI

Kutamanda kwa wolemba Masalimo kukuonetsa Chimwemwe chake mwa Mulungu. Dzifunseni nokha, Kodi ndimakondwera mwa Mulungu?

ANENERI: KULAMBIRA KULI NGATI KULENGEZA

Malamulo a nsembe, Hema ndi Kachisi amaonetsa kufunikira kwa mwambo mukulambira. Koma, aneneri akuonetsa kuti mwambo umene sukhala kulambira kwa mtima ndi wopanda kanthu. Anthu a ku Israeli anayamba kutsatira miyambo osakhala ndi mitima ya kumvera, aneneri anabweretsa uthenga wa chiweruzo. Analengeza kuti Mulungu sanalandirenso nsembe za mtundu woukira.

Aneneri akuonetsa kuti kulengeza kwa uthenga wa Mulungu ndi kulambira. Mu mwambo wathu wa mapemphero, tisamasiyanitse kulambira ku kulalikira. Kulalikira kwa Mawu ndi kulambira m'choonadi. Kulalikira kumatsimikizira ulamuliro wa Mulungu pa ife komanso nzeru zake za moyo wathu. Uku ndi kulambira; kumalemekeza Mulungu.

---

19 Charles Wesley, "Oh, For a Thousand Tongues." Accessed January 12, 2023. https://library.timelesstruths.org/music/Oh_for_a_Thousand_Tongues_to_Sing/

20 Martin Luther, tr. by Frederick Hedge, "A Mighty Fortress Is Our God." Accessed January 12, 2023. https://library.timelesstruths.org/music/A_Mighty_Fortress_Is_Our_God/

Uthenga wa Aneneri

Mwambo wosakhala ndi zenizeni sikulambira.

Amosi analengeza kuti Mulungu wakana nsembe za Israeli. Kodi ndi chifukwa chiyani? Khalidwe la wolambira linali lochimwa (Amosi 5:21-22). Yesaya analengeza kuti madyerero a Israeli anali otopetsa kwa Mulungu. Kodi ndi chifukwa chiyani? Chifukwa manja ake anali odzala ndi mwazi.

Kulambira kusanachitike, wolambira amalamulidwa: “Siyani kubweretsa nsembe zachabechabezo! Nsembe zanu zofukiza zimandinyansa Ine. Sindingapirire misonkhano yanu yoyipa, kapenanso zikondwerero za Mwezi Watsopano ndi Masabata. Zikondwerero zanu za Mwezi Watsopano ndi masiku anu opatulika ndimadana nazo. Zasanduka katundu wondilemera; ndatopa kuzinyamula. Mukamatambasula manja anu popemphera, Ine sindidzakuyang’anani; ngakhale muchulukitse mapemphero anu, sindidzakumverani. Manja anu ndi odzaza ndi magazi; sambani, dziyeretseni. Chotsani pamaso panu ntchito zanu zoyipa! Lekani kuchita zoyipa, phunzirani kuchita zabwino! Funafunani chilungamo, thandizani oponderezedwa. Tetezani ana amasiye, muwayimirire akazi amasiye pa milandu yawo” (Yesaya 1:13-17).

Mulungu sasunthika ndi miyambo imene sionetsera zoona zenizeni za mtima.

Kulambira koona kumafunika kudzipereka kwathu konse.

Abrahamu anapereka mwana wake kwa Mulungu; anapereka chabwino. Abele anapereka zoyamba kubadwa za ziweto zake; anapereka zabwino zake. Levitiko anafuna zabwino mwa nyama zopereka nsembe. Davide anakana kupereka nsembe imene siinamupangire mtengo wina ulionse (2 Samueli 24:24). Pa china chilichonse, kulambira kumafuna zabwino zathu.

Uthenga uwu ukupitirira mwa aneneri. Malaki anachenjeza za kubweretsa nyama zolumala za nsembe (Malaki 1:6-8) Haggai anachenjeza za chiweruzo chifukwa anthu anasamala za nyumba zawo osati nyumba ya Mulungu (Haggai 1:8-11). Kulambira koona kumafuna zabwino zathu.

Kulambira koona kumafuna moyo wathu onse.

Amosi anapereka yankho lodziwika zakupanduka kwa Israeli. Kuthetsa kwake sikunali nsembe zochuluka koma moyo wolungama. “Koma chiweruzo cholungama chiyende ngati madzi, chilungamo ngati mtsinje wosaphwa!” (Amosi 5:24). Aneneri samatsutsidwa ku

kulambira kwa mu Kachisi ndi nsembe.[21] Amatsutsidwa pa kulambira komwe kunalibe umoyo wa chilungamo.

Mu Baibulo monse tikuona kuti kulambira koona kumafuna moyo wathu onse. Mu mabuku asanu oyambilira a Baibulo, malamulo a kulambira ndi oyandikana ndi khalidwe; palibe kusiyana pakati pawo. Mu mabuku a mbiri, kusamvera kwa kwa moyo wa Israeli wa tsiku ndi tsiku ukuthera ku chionongeko cha malo olambirako a Israeli chifukwa cha kusamvera kwake. Mu Chipangano Chatsopano, Yesu akukumbutsa Afarisi kuti miyambo ya kulambira monga kutsatira Sabata sikunatanthauze kanthu popanda moyo wachifundo (Mateyu 12:7).

Chitsanzo cha aneneri: Kulalikira ndi Kulengeza ndi Kulambira

Aneneri akuonetsa kuti kulengeza Mawu a Mulungu kuti ndi kulambira. Taganizirani kupanda pake kwa Yeremiya kuima patsogolo pa Kachisi ndi kunena kuti "Pitani mu Kachisi ndikuyimba Masalimo ndi kupereka nsembe zanu. Kumeneku kukhala kulambira. Mukamaliza, ndilalikira uthenga wa Mawu a Mulungu kwa inu." Ayi! Kulengeza kwa Yeremiya kwa paokha unali mchitidwe wa kulambira. Yeremiya analalikira kuti Mulungu anakana kulambira kwa Israeli chifukwa cha miyoyo yawo ya uchimo. Uku kunali kulambira. Kunazindikiritsa kuyera kwa Mulungu Woyera; kunazindikiritsa kuyenera kwa Mulungu.

KULAMBIRA KWA BAIBULO LERO

Mipingo ina imasiyanitsa kulambira ndi kulalikira. Amalengeza, "Tiyamba ndi nthawi yakulambira." Kulambira kukatha, amalowa mu ulaliki. Izi zili ndi ziopsezo ziwiri.

1. Zikutanthauza kuti kulambira kuli ndi kulekezera pa nyimbo. Mtundu uwu wakulambira umakhazikika pa maimvaimva. Kulambira koona kuyenera kuposa maimbidwe.

2. Kumasiyanitsa kulengeza ndi kulambira. Chilichonse chimene timachita pa mwambo wakulambira wa mapemphero mu tchalitchi chiyenera kukhala kulambira. Nyimbo, pemphero, malemba, uthenga ngakhale chopereka ndi mbali ya kulambira.

---

21 Ophunzira ena amati aneneri anakana ndondomeko za kulambira za M'kachsi. Komabe, aneneri ambiri anali okhudzidwa kwambiri ndi Kachisi. Yesaya anaona Yehova mu Kachisi. Ezekieli ananenera za kubwezerezedwa kwa Kachisi wodzala ndi ulemelero wa Mulungu. Haggai analimbikitsa Zerubabele kuti amangenso Kachisi. Aneneri sanakane nsembe; anakana kugwiritsa ntchito mosayenera kwa nsembe.

FUFUZANI

Dzifunseni nokha, “Kodi kulalikira kwanga ndi m’chitidwe wa kulambira? Ndikamalalikira, kodi ndimayankhula ngati mthenga wa Mulungu amene akulemekeza Mulungu koyenerera”?

ZIOPSEZO ZA KULAMBIRA: KULAMBIRA KOSALINGANIZIKA

1. Kuopsa kwa kulambira mwa chizolowezi

Tikaiwala kuti kulambira kwa Baibulo kumafuna kudzipereka, tikhoza kumatenga Mulungu ngati mzathu chabe amene salandira ulemu. Kulambira kopanda mwambo kukhoza kulimbikitsa maganizo amenewa. Tisamaiwale kuti Mulungu ndi Mulungu odabwitsa amene amafunika kudzipereka konse kwathunthu. “Tsopano kwa Mfumu yamuyaya, yosafa, yosaoneka, amene Iye yekha ndiye Mulungu” (1 Timoteyo 1:17). Mipingo ina amaiwala kukula kwa Mulungu; kulambira kumachepetsedwa kuposa kumwa kapu yakhofi ndi mzawo.

2. Kuopsa kwa kulambira mwa chigulugulu

Tikaiwala kuti kulambira kwa mwambo ndi kulambira kwa Mulungu amene amafuna kumanga ubale ndi ife, tikhoza kuyamba kumutenga Mulungu ngati Mulungu amene ali patali. Kulambira kwa Mulungu kwa mwambo kukhoza kulimbikitsa maganinzo awa. Mipingo siilola mwayi uwu kuti okhulupirira akhale chifupi ndi Mulungu; chidwi chawo chonse chili pa mphamvu ndi ukulu wake.

Mu kulambira, tiyenera kuona ulamuliro wa mphamvu pa chilengedwe chake komanso chikondi chake ndi ana ake.

FUFUZANI

Ganizirani za mwambo wakulambira kwanu kwaposachedwa. Dzifunseni nokha, "Kodi ndi mbali iti yakulambira imene inalimbikitsa wolambira kuti alemekeze ukulu wa Mulungu? Kodi anachoka mu mwambo wamapemphero ndi maganizo a Mulungu wamkulu?" Kenaka dzifunseni nokha, "Kodi ndi ati amene analimbikitsa wolambira kumva ubale wapafupi wa Mulungu? Kodi anatuluka mu mwambo wakulambira akudziwa kuti Mulungu amawakonda?"

KUMALIZA: UMBONI WA OWONA NDI MASO KUPEREKA KWA KACHISI

Kodi zikanakhala zotani kukhala pa mwambo wa kupereka Kachisi? Mwina zikanafotokozeredwa motere:

"Ndinaliko kumwambo wa kupereka Kachisi. Sindidzaiwala tsiku limenelo. Tinakhala tikudikira mwambo umenewu kwa zaka zambiri.

"Zaka? Inde, zaka! Mfumu Davide anapanga mapulani omanga Kachisi ndipo anawapatsira kwa Solomoni asanamwalire. Tsopano Kachisi anamalizika, ndipo mwambo wopereka wakachisi oyembekezereka kwa nthawi yaitali unachitika.

"Unali mwambo wokonzedwa bwino ndi opatsa chidwi. Taganizani…

- Kupereka nsembe kwa ngo'mbe 22,000 komanso nkhosa 120,000
- Kwaya ya mazana ikuimba Masalimo a Davide
- Gulu loimba malipenga, azeze zitoliro
- Ansembe ndi Alevi atavala mikanjo yoyera kwambiri
- Chimodzi mwa zimango zokongola kwambiri zimene zinamangidwapo
- Zipangizo za golide ndi siliva za kulambira kulikonse

"Unali mwambo wokongola, koma ubwino kukongola kwa mwambo sikumene kuli kofunikira kwambiri mukukumbukira kwanga. Zimene ndikukumbukira kwambiri oyimba anayamba kuyimba zida ndikuyamba kuyimba, 'ulemelero wa Yehova unadzadza nyumba ya Mulungu kufikira ansembe sanathenso kutumikira ntchito zawo. Kutumikira **kwa** Mulungu kutengedwa **ndi** Mulungu!

“Papita zaka zambiri chichikireni mwambo okumbukirika umenewu. Sindikunena kuti mwambo ulionse umene ndakhalapo kuyambira tsiku limenelo umakhala ndi zizindikiro zooneka zofanana za kupezeka kwa Mulungu; limenelo linali tsiku lapadera. Komabe mwambo uliwonse umene ndimapezekapo, ndimayembekezera kupezeka kwa Mulungu.

“Nthawi zina, kupezeka kwake ndikodabwitsa, kumakhala kwachete. Nthawi zina kupezeka kwake kumamveka m’maimbidwe; nthawi zina amayankhula kudzera muuthenga. Nthawi zina, maimvaimva anga amakhudzika; nthawi zina, choonadi chake chimayankhula ku moyo wanga. Ndimakhala olimbikitsika; nthawi zina, ndimakhala otsutsika.

“Pakusatengera m’mene Mulungu amasankhira kuti apezekere, ndimalemekeza kupezeka kwake. Mwina sindingaonenso kupezeka kotero kwa Mulungu kooneka ndi maso, koma ndikhoza kulowa mu kupezeka kwake nthawi ina iliyonse ndi kulambira.”

KUKAMBIRANA KWA GULU

» Kuti phunziro ili limveke bwino, kambiranani izi:

Esitere ndi M’khristu wokhulupirika ndipo amakonda kupita ku mwambo wakulambira m’mudzi mwawo. Nyimbo zamphamvu komanso chiyanjano kumabweretsa kusintha kolandirika kuchoka ku zovuta za moyo wa tsiku ndi tsiku. Amakonda zimene amamva ndi maimvaimva amene amakumana nawo akamalambira Mulungu ndi mtima wake onse. Komabe, Esitere, amaziona zovuta kuika luntha lomwelo mu banja lake komanso ntchito za tsiku ndi tsiku limene Amachita mu m’mawa wa kulambira kwa tsiku lasabata. Kodi Esitere mungamupatse uphungu otani?

KUBWEREZA KUONANSO PHUNZIRO 3

1. Mulungu amasamala m’mene timalambirira chifukwa:

- Kalambiridwe kathu kamakhudza kumvetsetsa kwathu kwa Mulungu.
- Kalambiridwe kathu kamaonetsa chifukwa chimene timalambirira.

2. Kulambira ndi ubale – kuyenda ndi Mulungu.

- Mulungu anapereka njira za kalambiridwe kwa Adamu ndi Hava.
- Mulungu anatengapo mbali kupangitsa kulambira kukhala kotheka kwa Abrahamu.
- Chisomo cha Mulungu chinapangitsa kulambira kukhala kotheka kwa Yakobo.
- Tikamayankhula ndi Mulungu, miyoyo yathu imasinthika.

3. Kulambira kumayamba ndi kumvera.

   - Kulambira kumayamba ndi kumvera. Kulambira kumaposa maimvaimva kapena kumva.
   - Kulambira ndikuvomera kwa machitachita ku malamulo a Mulungu.
   - Kumvera Mulungu kumazamitsa ubale wathu ndi Iye.

4. Kulambira kumakhala ndi mwambo (nsembe za Chipangano Chakale).

   - Nsembe zinaimira kumvera kwathunthu kwa Mulungu (Aroma 12:1).
   - Mulungu analemekeza kulambira koona ndi kupezeka kwake (2 Mbiri 5).
   - Mwambo wagulu uyenera kuchokera mu mtima wakumvera.

5. Kulambira kumakhala ndi matamando (Masalimo).

   - Buku la Masalimo limaonetsa kuti kulambira kumaphatikizana ndi kutamanda.
   - Buku la Masalimo limaonetsa kuti kulambira kumaphatikizana ndi kulira.

6. Kulambira kumaphatikiza kulengeza (aneneri).

   - Kulambira ndikoposa kutamanda; ndikulengezanso kwa choonadi. Kulalikira ndi kulambira.
   - Aneneri anaphunzitsa kuti mwambo wopanda zenizeni sikulambira.
   - Aneneri anaphunzitsa kuti kulambira koona kumafuna zabwino zathu.
   - Aneneri anaphunzitsa kuti kulambira koona kumafunika zonse za moyo wathu onse.

NTCHITO YA PHUNZIRO 3

1. Tchulani mfundo zitatu za kulambira zimene mwaphunzira kuchokera muphunziro ili pa kulambira kwa Chipangano Chakale. Lembani tsamba limodzi limene mufotokonzere njira yodziwika yogwiritsira ntchito mfundo iliyonse yakulambira kwa mpingo wanu.

2. Pachiyambi chaphunziro lotsatira, mudzalemba mayeso a phunziro ili. Werengani mafunso a mayeso mosamala pakukonzekera.

MAYESO A PHUNZIRO 3

1. Kuchokera pa phunziro ili, tchulani zitsanzo ziwiri za kulambira kwa Baibulo kumene kunakanidwa ndi Mulungu.

2. Mawu akuti *anayendabe ndi Mulungu* akuwonetsa kuti kulambira koona kumakhala _____ ndi Mulungu.

3. Kuchokera mu phunziro ili, nenani anthu atatu osayenera amene Mulungu mwachisomo anawapatsa kuthekera kwa kumulambira iye.

4. Nsembe ya Abrahamu ya kupereka Isake ikuonetsa kuti kulambira kowona kumafunika _____ kwa thunthu.

5. Kodi kusiyana kwa kulambira kwa Abele ndi kulambira kwa Kaini ndi kotani?

6. Kodi kufunikira kwa wolambira kusanjika manja pa mutu pa nyama yoperekedwa nsembe kunali kotani?

7. Mu Buku la Masalimo, muli mitundu iwiri ya kuyamika. Kuyamika kwa chikhalidwe komanso ntchito zamphamvu za Mulungu kumatchedwa _____ kofotokonzera. Kuyamika kumene kulibe chindunji kumatchedwa _____ kwa kulengeza.

8. Aneneri akuonetsa kuti _____ cha uthenga wabwino ndi kulambira.

9. Tchulani maganinzo atatu a uthenga wa aneneri pa zakulambira.

10. Tchulani zinthu ziwiri zoopsa zosagwirizana mu kulambira.

11. Lembani Mika 6:6-8 kuchokera pakuloweza.

PHUNZIRO 4

KULAMBIRA MU CHIPANGANO CHATSOPANO

ZOLINGA ZA PHUNZIRO

1. Kuzindikira m'mene Yesu anakwaniritsira Kulambira.
2. Kuchokera mu mabuku a Uthenga wabwino, Machitidwe ndi Chivumbulutso, zindikirani mitundu yabodza ya kulambira.
3. Pangani chisankho cha panokha pa kulambira ndi kufalitsa uthenga.
4. Kuchokera m'makalata, dziwani zinthu zoyambirira za Kulambira mumpingo woyamambirira.
5. Onani kulambira kumene kumakhazikika pa Mulungu.

KUKONZEKERA PHUNZIRO ILI

Lowezani Aroma 12:1-2.

CHIYAMBI

Abusa a James, Enoch, Gideon ndi Jason anakumananso kuti akambirane zimene aphunzira za kulambira kuchokera mu Chipangano Chakale.

James, amene amalemekeza kulambira kwachikhalidwe anati, "Ndikuganiza kuti Chipangano Chakale chikutsimikizira kuti

"Kulambira ndi chinthu chapamwamba komanso chinthu chokhacho chofunikira kwambiri cha mpingo wa Chikhristu, chokhacho chidzakhalapo... mpaka kumwamba pamene zinthu zonse za mpingo zitatha."

W.Nicholls

mpingo wanga ukuchita kulambira moyenera. Kulambira kwa M'kachisi kunali kokhazikika ndi kwadongosolo. Izi ndi zimene timayesetsa kuchita."

Enoch anaseka, "Zoona, koma kodi munawerenga zimene ananena aneneri? Mwambo wa kulambira wa Kachisi sunatanthauze kanthu! Kulambira kumene kumasangalatsa Mulungu ndikulambira kumene kumachokera mumtima. Ndi zimene timachita mukupempedza kwamakono; tikukhudza mitima ya m'badwo watsopano."

Mwakukhumudwa, Gideon anati, "Sitilinso patali ndi paja tinayambira phunziro lathu la kulambira. Kodi bwanji Mulungu sangangonena kuti, 'Umu ndi m'mene muyenera kulambirira Ine?"

Jason anayankhula. "Tisagonje. Ndife a Khristu a Chipangano Chatsopano; mwina Chipangano Chatsopano chiyankha mafunso athu. Tiyeni tiphunzire Kulambira mu Chipangano Chatsopano ndikuona zimene chimanena."

» Kodi kulambira kunasintha motani mu Chipangano Chatsopano? Kodi kulambira kwa mpingo woyambirira kukusiyana motani ndi kulambira kwa M'hema ndi Kachisi? Fotokozani mwachidule za zimene mukudziwa kale za kulambira kwa Chipangano Chatsopano.

MABUKU A UTHENGA WABWINO: KULAMBIRA KUMAKWANIRITSIDWA MWA YESU KHRISTU

Theka la Chipangano Chatsopano kuwoneka kwa liwu la *Kulambira* kuli M'mabuku a Uthenga Wabwino. Mabuku a Uthenga Wabwino amawonetsa kuti Yesu ndiye kukwaniritsa kwakukulu kwa kulambira. Amakwaniritsa kulambira munjira ziwiri.

1. Mu umunthu wake, Yesu anapereka chitsanzo cha kulambira.
2. Mu umulungu wake, Yesu akulambiridwa.

Mu Umunthu Wake, Yesu Anali Chitsanzo Chachikulu Cha Kulambira

Yesu anapereka chitsanzo cha kulambira kowona. Yesu anauza mzimayi wa ku Samariya kuti Mulungu akufuna amene amamulambira Iye mu mzimu ndi m'choonadi (Yohane 4:24). Mu mwambo wake wakulambira (Kuwerenga Baibulo, pemphero, kupita ku sunagoge ndi Kachisi), Yesu anaonetsa zimene zimatanthauza kulambira moona mumzimu ndi m'choonadi.

Yesu anakonda malo wolambirapo.

Luka akuonetsa chikondi cha Yesu cha malo a kulambira. Ngakhale ngati mwana, Yesu analemekeza Kachisi ngati nyumba ya Atate wake (Luka 2:41-49). Anali ndi kukhudzika

ndi chiyero cha Kulambira kwa Kachisi; Maulendo awiri anathamangitsa amene amachita zosayenera mu Kachisi.[22]

Koyambirira kwa utumiki wake, Yesu anapita ku sunagoge mu Nazareti pa tsiku la Sabata monga m'mene mwambo wake unalili (Luka 4:16). Mu utumiki wake onse wa padziko, Yesu nthawi zambiri anapita ku sunagoge.

Yesu anakana kulambira wina aliyense kapanena china chilichonse koma Mulungu.

M'chipululu, Yesu anakana yesero la kulambira kwabodza.

» Werengani Mateyu 4:9-10.

Yesero la kulambira cholengedwa osati Mlengi ndi mutu waukulu wa nkhani m'malemba monse. Ndi muzu wakulambira mafano mu Chipangano Chakale. Chivumbulutso amaonetsa kusiyana pakati pa kulambira kwa chinjoka ndi chilombo, ndi kulambira kwa Mulungu ndi Mwana wa Nkhosa. Yesu anakana kulambira cholengedwa.[23]

Yesu anapemphera mwachikhalidwe.

Pemphero linali lofunikira mu utumiki onse wa Yesu. Maulendo khumi ndi asanu, mabuku a Uthenga Wabwino amanena kuti Yesu anapemphera. Pa zina mwazochitikazi, anakhala usiku onse yekha ndi Atate Ake. Asanasankhe ophunzira khumi, anakhala usiku onse mupemphero (Luka 6:12). M'maola ake omaliza okhala ndi ophunzira, Yesu anapempherera ophunzira komanso amene adzakhulupirira m'tsogolo (Yohane 17). Ataona mtanda, anapita Getsmane kukapemphera (Mateyu 26:36-42. Pemphero linali lofunikira mu Kulambira kwa Yesu.

Yesu anafotokozera kulambira koona.

Pakuwonjenzera kupereka chitsanzo cha kulambira kudzera mu zochita zake, Yesu mosalekeza anaphunzitsa za kulambira. Anaphunzitsa mzimayi wa ku Samariya za kulambira koona. Yesu anaphunzitsa pemphero la chitsanzo kudzera m'mafaninzo (Luka 11:5-8, Luka 18:1-14).

» Werengani Luka 11:1-4.

Pemphero la Yesu la chitsanzo likuonetsa kuti pemphero liyenera kuchokera mu mtima wa kulambira. Pemphero likuyamba ndi, "Dzina lanu liyeretsedwe." Kuyeretsa ndi kulemekeza ngati woyera. Mu pemphero, timamutenga Mulungu ngati woyera.

---

22 Yohane 2:13-16 amanena za kuyeretsa koyamba. Mateyu 21:12-27, Marko 11:15-17, ndi Luka 19:45-46 amanena za kuyeretsa kwachiwiri mu sabata yomaliza ya utumiki wake wa padziko.

23 Yesu sanali ngati anthu amene ananendwa pa Aroma 1:25.

Yesu anadzudzula kulambira kwabodza.

Ngati kulambira koona ndi kulambira mumzimu ndi m'choonadi, kulambira kwabodza ndi kwina kulikonse kumene sikufikira apa. Yesu anakana:

1. Kulambira kodzikweza

Pa uthenga wa paphiri, Yesu anachenjeza kuti ndizotheka kuchita zinthu zabwino ndi zolinga zolakwika. Kupereka kwa osauka, pemphero, komanso kusala zonse izi ndi zizindikiro za kulambira koona. Yesu anachenjeza iwo amene izi kuti awoneke kwa ena; ndi odzikweza (Mateyu 6:1-18). Wolambira owona amachita izi mwakufuna kulambira Mulungu.

Pa Mateyu 23, Yesu anatsutsa atsogoleri a chipembedzo amene amaphunzitsa zinthu zoona za kulambira, koma mitima yawo ili kutali ndi Mulungu. Yesu anati ziphunzitso zawo ndi zoona, koma mitima yawo inali yolakwika; ndipo ndi achinyengo.

2. Kulambira kwa chilamulo

Choopsa china ndi kulambira kodzikweza; kulambira kufuna kudzionetsera kwa owona osati kukondweretsa Mulungu. Choopsa china ndi chilamulo; kulambira kofuna kupeza chisomo cha Mulungu pakukwaniritsa zoyenereza zina. Tikafuna kupeza chisomo cha Mulungu pa machitidwe athu a kulambira, timataya zoona zenizeni za kulambira koona. Kulambira kumakhala ntchito imene timapezapo kovemereza kwa Mulungu m'malo mwakuvomereza kwa chimwemwe ku ubwino wa Mulungu.

Yesu anakhumudwitsa atsogoleri a chipembedzo a Israele pamene pamene anaphwanya miyambo yawo.[24] Yesu sanaononge lamulo ngakhale mzimu wa chilamulo; anaononga miyambo ya anthu imene inakhazikika kwazaka zambiri za chilamulo cha Afarisi. Kwa Afarisi, miyambo inali yofunikira Ngati lamulo palokha. Anakhukupirira kuti kutsatira lamulo kunapezetsa chisomo ndi Mulungu. Izi zikutanthaunzira chilamulo: Kufuna kupeza chisomo cha Mulungu pakukwaniritsa zoyenereza. Yesu anakana chilamulo molimba monga m'mene anakanira kudzikweza.

Mu Umulungu Wake, Yesu Akulambiridwa

Pambuyo pa kufa ndi kuuka kwake, **Yesu amakhala kudzanja lamanja la Atate ndipo akulandira kulambira moyenera** (Chivumbulutso 5:12-14). Paulo analemba za kusinthika uku mu Afilipi 2. Chifukwa cha kudzichepetsa yekha kodzipereka, tsopano ndi wokwezedwa komanso kulambiridwa.

> Choncho Mulungu anamukweza Iye kukhala wapamwamba kwambiri, ndipo anamupatsa dzina loposa dzina lina lililonse kuti pakumva dzina la Yesu, bondo

24 Mateyu 12:1-14, Luka 13:10-17, ndi Yohane 5:8-18, ena mwa iwo.

lililonse limugwadire, kumwamba ndi pa dziko lapansi ndi pansi pa dziko, ndipo lilime lililonse livomereze kuti Yesu Khristu ndi Ambuye kuchitira ulemu Mulungu Atate (Afilipi 2:9-11).

Pa Mateyu 18:20, Yesu anachitira umboni kuti ndiwoyenera kulambira. Mu chikhalidwe cha Chiyuda, amuna khumi amafunika sunagoge Asanakumane ku mapemphero komanso kulambira. Yesu ananena kwa ophunzira ake, "Pakuti pamene awiri kapena atatu asonkhana pamodzi m'dzina langa, Ine ndili nawo pomwepo." Mu mpingo **Kupezeka kwa Yesu, osati chiwerengero cha anthu, ndi chimene chimapangitsa kalambira kutheka**.

Kudzera mu zotsatira zake khamu la anthu amene anaona zozizwa zake, Yesu akuonetsa kuti ndi oyenera kulambira. Ataona zozizwa zake, **anthu analemekeza Mulungu**, m'chitidwe wa kulambira. Anthu amene anaona machiritso ake onse anazizwa (Marko 1:23-27).

Mu usiku wake womaliza ndi ophunzira, Yesu anadya Pasaka. Pamene chakudya ichi chinatsatira khalidwe la Chiyuda la chakudya cha Pasaka, Yesu anachipatsa tanthauzo latsopano pamene anauza ophunzira ake kuti mkate ndipo Iye anatenga buledi, nayamika ndipo anamunyema, nagawira iwo nati, "Ili ndi thupi langa lomwe laperekedwa kwa inu; muzichita zimenezi pokumbukira Ine." Chimodzimodzinso, utatha mgonero, anatenga chikho nati, "Chikho ichi ndi pangano latsopano la magazi anga, amene akhetsedwa chifukwa cha inu" (Luka 22:19-20).

» Werengani Luka 22:13-20.

Anawalamula kuti azichita izi ngati chikumbutso chake. **Mgonero wa Ambuye umalunjika pa Khristu, kukwaniritsa kwabwino kwa Pasaka**.

KULAMBIRA KWA BAIBULO LERO

Kudzudzula kwa Yesu kwa kulambira kwabodza ndi chitsanzo chake cha kulambira koona kumaonetsa kuti kulambira kwathu kuyenera kukhale koona, osati chifukwa chofuna kuonekera kwa ena. Kulambira koona kuyenera kukhale kofuna kukondweretsa Atate, osati kukondweretsa ena.

Ili ndi yesero lokhazikika kwa atsogoleri a mpingo. Chifukwa chakuti kulalikira komanso kulambira kumachitika pagulu, tikhoza kuyesedwa ndi machitidwe osati kulambira. Tikakhazikika pa kusangalatsa gulu osati kulemekeza Mulungu, timachita chionetsero osati kulambira.

Kodi ndi yesero lotani la kupembedza kwabodza kwa mtsogoleri?

- Ndime ya uthenga yosankhidwa chifukwa tikudziwa kuti ndiyotchuka kwa anthu
- Pemphero limene limayankhula kwambiri kwa wolambira osati kwa Mulungu

- Chopereka chimene chimaperekedwa mwa njira yopereka chidwi kwa opereka
- Nyimbo zimene zimabweretsa chidwi kwa woyimba osati kwa Mulungu

Chiphunzitso komanso chitsanzo chimene cha Yesu chimatikumbutsa kuti kulambira koona ndi kwa Mulungu yekha. Kulambira ndi kwa iye, osati kwa ife.

FUFUZANI

Dzifuseni nokha, "Kodi ndi ndani amene amalemekezedwa mu utsogoleri wanga wa kulambira? Kodi ndimalalikira, kuimba kupemphera, komanso kupereka kumene kumabweretsa ulemerero wa Mulungu, kapena kapena kudziwika kwanga? Kodi ndikulambira moona?"

MACHITIDWE: KULAMBIRA NDI ULALIKI

Kulambira ndi kogwirizana kwambiri ndi ulaliki. Osakhulupirira amakhala olambira akamva ndi kulandira uthenga. Machitidwe amaonetsa kulumikizana pakati pa kulambira ndi kulalikira.

Yesaya 6:8 amaonetsa kuti kulambira kumathera kukulambira; kumvomera kwa Yesaya ku kulambira kunali kwakuti kenaka ndinamva mawu a Ambuye akuti, "Kodi ndidzatuma yani? Ndipo ndani adzapite m'malo mwathu?" Ndipo ine ndinati, "Ndilipo. Tumeni!" Tikamalambira moona, timakhala ndi kukhudzika kwa kulambira. Mu kulambira, timaona Mulungu komanso zosowa za dziko lathu kudzera m'maso a Mulungu. Kulambira kumapanga alaliki.

Kulambira kumalimbikitsa mpingo ku ulaliki. Ngati mpingo utsogolera osakhulupirira kwa Khristu, okhulupirira atsopano amakhala wolambira. Wolambira atsopano amalimbikitsika ndi ulaliki.

Machitidwe amaonetsa ndondomeko ikuchitika. Paulo atalalikira kwa Aefeso, anthu anatembenuka kuchoka kwa Atemi ndi kulambira mafano opangidwa ndi manja kupita kukulambira kwa Mulungu owona (Machitidwe 19:26-27). Pamene tikulalikira Khristu, okhulupirira atsopano amabwera ku ufumu; amakhala wolambira. Ulaliki umapanga wolambira.

Kulambira Koona Kumalimbikitsa Kufalitsa Uthenga Wabwino



Machitidwe amayamba ndi ophunzirra akulambira; anali ndi cholinga chimodzi kudzipereka okha ku pemphero (Machitidwe 1:14). Machitidwe akuthera ndi Paulo akulakira ku Roma; "Molimba mtima ndi popanda womuletsa, Paulo analalikira za ufumu wa Mulungu ndi kuphunzitsa za Ambuye Yesu Khristu" (Machitidwe 28:31).

Kulambira kwa Akhristu oyambirira kunathera ku ulaliki. Kuitanidwa kwa Paulo ndi Barnaba kunachitika pa kulambira.

> Iwo pamene ankapembedza Ambuye ndi kusala kudya, Mzimu Woyera anati, "Mundipatulire Barnaba ndi Saulo kuti akagwire ntchito imene ndinawayitanira." Ndipo atasala kudya ndi kupemphera anasanjika manja awo pa iwo nawatumiza (Machitidwe 13:2-3).

Kulambira koona kumalimbikitsa kufalitsa uthenga wabwino.

Kufalitsa Uthenga kwa Mphamvu Kumapanga Wolambira

Mu Machitidwe yense, ophunzira anakhala mu kulambira. Pa Pentekoste, anthu 3,000 anapulumutsidwa. Okhulupirira atsopano anakhala wolambira; Iwo anasonkhana pamodzikuphunzitsidwa ndi atumwi pa chiyanjano, chakudya ndi popemphera (Machitidwe 2:42).

» Werengani Machitidwe 2:42-46 kuti muone chithunzi cha kulambira mu mpingo woyambirira.

Akhristu a Chiyuda anapitiriza kupemphera mu Kachisi.[25] Kuonjezera apo Akhristu a Chiyuda ndi a Mitundu amakuma mu sunagoge kukalambira. M'mizinda yambiri, Paulo amayamba utumiki wake mu sunagoge, kuonetsera Yesu ngati kukwaniritsa kwa malonjezano a Chipangano Chakale.[26] Kulambira kumachitikanso m'nyumba. Tsiku ndi tsiku amkasonkhana pamodzi pabwalo la pa nyumba kuchita chiyanjano ndi kulambira (Machitidwe 2:46). Makalata a Paulo ali ndi moni wopita ku mipingo yosonkhana m'nyumba.[27] Kufikira anthu mwa ulaliki kwa mpingo woyambirira kunapanga thupi latsopano la wolambira.

25 Machitidwe 2:46, Machitidwe 3:1, 11-26; Machitidwe 4:2, Machitidwe 5:12, 42.

26 Machitidwe 13:14-15, Machitidwe 14:1, Machitidwe 17:1, 10; Machitidwe 18:4, 19; Machitidwe 19:8.

27 Aroma 16:5, 1 Akorinto 16:19, Akolose 4:15, Filimoni 1:2.

Ulaliki pa Mars Hill

Uthenga wa Paulo ndi uthenga wa pamwamba umene ukuonetsa kugwirizana pakati pa ulaliki ndi kulambira (Machitidwe 17:16-34). Ku Atene, Paulo analimbana ndi chikhalidwe chimene chinali chodzala ndi kupembedza mafano. Paulo anaonetsa kusiyana kwa pakati pa kulambira kwabodza kwa mafano ndi kulambira koona kwa Yehova.

Anthu a ku Atene anali a chipembedzo (Machitidwe 17:22)

Anthu a ku Atene anali wolambira, koma sanalambire Mulungu woona. Kulambira kwawo kunali kwabodza. Kulambira kwapokha sikokwanira; kulambira kumafunika kuzilunjika kumalo koyenera.

Anthu a ku Atene anapembedza mwa kusadziwa (Machitidwe 17:23).

Sanadziwe amene anamulambira. Paulo analengeza za Yehova amene anakhala akumufuna. Anawauza kuti Mulungu anapanga mitundu yonse kuti amve mamvekedwe otere kwa Iye ndi kumupeza. Ili ndi liwu limene likuonetsa wina wake amene akusokera mu mdima. Njala ya munthu pa Mulungu inapereka khomo la uthenga wabwino.

Anthu a ku Atene analambira Mulungu osaziwika.

Yehova salambiridwa ndi manja a anthu, ngati kuti amafuna china chilichonse. Iye ndiye amene amapereka moyo, mpweya ndi zinthu zonse kwa anthu (Machitidwe17:25). Kulambira kwa anthu a ku Atene kunali kwabodza chifukwa chakuti mulungu wawo anali wosakwanira. Mulungu owona amapereka moyo kwa onse; sasoweka kanthu. Timalambira Mulungu chifukwa amayenera kulambira kwathu, osati kuti amasowekera kulambira kwathu.

Paulo anasiyanitsa mafano ndi Mulungu owona.

1. **Mulungu ndi Mlengi.** Mulungu amene analenga dziko lapansi ndiponso zonse zili m'menemo ndiye Ambuye wakumwamba ndi dziko lapansi (Machitidwe 17:24). Gulu la Aepikureya ndi Astoiki, anthu anzeru, anayamba kutsutsana naye. Ena a iwo anafunsa kuti, "Kodi wolongololayu akufuna kunena chiyani?" Enanso anati, "Akuoneka ngati akulalikira milungu yachilendo." Iwo ananena zimenezi chifukwa Paulo amalalikira Uthenga Wabw (Machitidwe 17:18) ndi Mlengi wa dziko lonse.

2. **Mulungu ali pafupi.** Mulungu anachita izi kuti anthu amufunefune, ndikuti pomufunafunapo amupeze ngakhale kuti Iye sali kutali ndi aliyense wa ife (Machitidwe 17:27). Ngakhale Mulungu ali kutali, koma analowa m'dziko lathu ndipo ali pafupi ndi wolambira aliyense.

3. **Mulungu adzaweruza amene amakana kulapa** (Machitidwe 17:30-31). Kulambira m'choonadi kumazindikira kuti Mulungu ndiye Oweruza olungama amene sadzalola kuukira. Mu kulambira kwathu, timadzipereka tokha ku ukulu wake.

4. **Mulungu anaukitsa Yesu kwa akufa, kuonetsa kuti Yesu ndi oyenera kulambira** (Machitidwe 17:31). Yesu modzipereka anadzichepetsa yekha kufikira ku imfa; tsopano wakwezedwa ndi Atate, "kuti pakumva dzina la Yesu, bondo lililonse limugwadire, kumwamba ndi pa dziko lapansi ndi pansi pa dziko, ndipo lilime lililonse livomereze kuti Yesu Khristu ndi Ambuye kuchitira ulemu Mulungu Atate" (Afilipi 2:10-11).

Uthenga wa Paulo kwa Atene unalimbana ndi kulambira kwabodza kwa mafano ndi uthenga wa kulambira koona kwa Yehova. Ulaliki wamphamvu umapanga wolambira.

ZIOPSEZO ZA KULAMBIRA: KULAMBIRA KOPANDA ULALIKI

Mipingo yambiri imalekanitsa kulambira ku utumwi ndi ulaliki. Mipingo ina imati, "Ndife odzipereka ku ulaliki. Cholinga chathu ndi kufikira otaika." Mipingo imeneyi imapereka chidwi chochepa ku kulambira. Amadziona wokha ngati mipingo yolalikira. Mipingo ina imati, "Timakhulupirira kuti cholinga choyambirira cha mpingo ndi kulambira. Anthu ena akhoza kuchita ulaliki; cholinga chathu ndi kulambira."

Machitidwe akuonetsa kuti mpingo uyenera kudzipereka ku zonse ku kulambira **ndi** kulalikira. Kulambira koona kumatipatsa kukhudzika kochita ulaliki. Ulaliki wamphamvu umapanga wolambira a tsopano.

Tisamalekanitse kulambira ku ulaliki. Kulambira kumene sikulimbikitsa ulaliki ndimwachidziwikire kudzakhala kulambira kodzikundikira kumene kumachitika pofuna kudzilimbikitsa tokha. Ulaliki umene sutsogolera ku kulambira udzakuza a Khristu osazama amene amalephera kuona Mulungu moona.

Mukulambira kwa Baibulo, timapeza kukhudzika kwatsopano kwa kulaliki. Monga Yesaya, kuona kwathu kwa Mulungu kudzatifikitsa ife ponena kuti, "Ndilipano! Nditumeni."

FUFUZANI

Dzifunseni nokha, "Kodi kulambira kumatilimbikitsa kugawana uthenga wabwino ndi osakhulupirira? Kodi ndili ndi kukhudzika kobweretsa wolambira atsopano kwa Mulungu?"

MABUKU A MAKALATA: KULAMBIRA MU MPINGO WOYAMBIRIRA

Mosiyana ndi Chipangano Chakale ndi ndondomeko zake zapadera za kulambira kwa Chiyuda, Chipangano Chatsopano chimapereka ndondomeko zochepa za kulambira mu mpingo.[28] Palibe kufotokozera kwa thunthu kwa mwambo wa kulambira mu Chipangano Chatsopano, koma mabuku a makalata amaonetsa mfundo zina za kulambira kwa Chikhristu koyambirira.

Kuwerenga Mawu

Kuwerenga Malemba kunali kofunikira mu kulambira kwa Chikhristu koyambirira. Akolose 4:16 ndi 1 Atesalonika 5:27 akulangiza mipingo kuwerenga makalata a Paulo pagulu. Pa 1 Timoteyo 4:13, Paulo akukumbutsa Timoteyo kuti akhale ndi chidwi ku kuwerenga kwa malemba kwa pagulu.

Kufunikira kowerenga malemba kukuperekedwa pa Akolose 3:16, "Mawu a Khristu akhazikike kwathunthu m'mitima mwanu... ndi nzeru zonse." Wolemba Masalimo anafotokozera, munthu odala; kuti Chikondwerero chake chili m'malamulo a Yehova (Masalimo 1:2). Kulambira kwathu kwa pagulu kumaonetsa chidwi chimene timaika pa malemba.

Kulalikira Mawu

Kuphatikizapo ndi kuwerenga malemba, mtsogoleri anali ndi udindo wolalikira Mawu (2 Timoteyo 4:1-4, Tito 2:15). Kuyambira mu nthawi ya Ezara, alembi anatanthauzira anthu malemba. Ezara ndi anzake amawerenga kuchokera m'buku, kuchokera mu Chilamulo cha Mulungu, momveka bwino, ndipo amapereka nzeru, kuti anthu amvetsetse kuwerenga (Nehemiya 8:8). Masunagoge a Chiyuda mu nthawi ya Chipangano Chatsopano anapitirira ndi mchitidwe uwu (Machitidwe 13:14-15). Kupereka nzeru ya malemba ndi maziko a kulalikira kwa kwa Chikhristu koyambirira.

Mauthenga mu Machitidwe akuonetsa zopezeka mu kulalikira kwa Chikhristu koyambirira.[29] Mitu yofunikira mu ma uthenga awa muli:

- Yesu anali kukwaniritsa kwa mauneneri a Chipangano Chakale.
- Yesu anachita zinthu zamphamvu kudzera mu mphamvu ya Mulungu.
- Yesu anapachikidwa ndi kudzutsidwa kwa akufa.
- Yesu tsopano akukwezedwa ndipo anapangidwa kukhala Mbuye.
- Onse amene amamva alape ndi kubatizidwa.

---

28 Zambiri za izi zatengedwa kuchokera kwa Franklin M. Segler and Randall Bradely, *Christian Worship: Its Theology and Practice.* (Nashville: B&H Publishing, 2006), Chaputala 2.

29 Mauthenga ofunikira M'machitidwe amapezeka pa Machitidwe 2, 7, 10, 17.

Kupemphera Pagulu

Pemphero la pagulu linali lofunkira mu Kulambira kwa Chikhristu koyambirira (1 Timoteyo 2:1-3). Ophunzira ambiri amakhulupirira kuti mapemphero amene anaikidwa mu makalata a Paulo amagwritsidwa ntchito pa kulambira kwa pa gulu. “Ameni wagulu” anaonetsera kugwirizana kwawo ndi pemphero.[30]

Kuyimba

Kuyimba kunali kofunikira mu Kachisi ndipo kunapitirira kugwira ntchito mu kulambira kwa Chikhristu koyambirira. Kuphatikiza Masalimo amene a Khristu anabweretsa kuchokera ku kulambira kwawo kwa Chiyuda, nyimbo zambiri zinalemekeza Yesu ngati Mesiya. Izi zikuonedwa ngati za pa Aefeso 5:19 ndi Akolose 3:16. Ophunzira ambiri a Baibulo amakhulupirira kuti Afilipi 2:5-11 inali nyimbo yoyambirira ya Chikhristu. Pakuwonjezera, nyimbo ya Mariya pa Luka 1:46-41 ndi pemphero la Simioni pa Luka 2:29-32 zikhoza kukhala kuti zimayimbidwa mu mwambo wa kulambira.

Zopereka

Pazochitika zina, kupereka kunali mbali imodzi ya kulambira kwa pa gulu. 1 Akorinto 9:6-13 akulondolera mpingo kwa Akorinto kuti usonkhetse chopereka cha Akhristu ozunzika mu Yerusalemu.

Ubatizo ndi Mgonero wa Ambuye

Mwambo waubatizo ndi Mgonero wa Ambuye zinali mbali imodzi ya kulambira. Paulo analemba pakukonza zolakwika mu chikondwerero cha Akorinto cha Mgonero wa Ambuye. M’malo mokumbukira kudzipereka nsembe kwa Yesu, linasanduka phwando. Paulo anachenjeza za kufunikira kwa Mgonero wa Ambuye. Chiyanjano chimakumbukira mwambo wopatulika kwambiri kwa Akhristu; sichiyenera kutengedwa mopeputsidwa.[31]

Kupitirira pa zisonyezo izi za zindikiro za mwambo wa kulambira, timadziwa zochepa za kulambira koyambirira kwa Chikhristu. Mabuku a makalata safotokoza za ndondomeko ya padera ya kulambira kwa Chikhristu, kasungidwe ka kulambira, kapena ndondomeko zina za kulambira kwa pagulu mu mpingo woyambirira ndizachidziwikire kuti kulambira kwa pagulu kumaoneka mosiyanasiyana ku malo osiyanasiyana. Akhristu a Chiyuda mwina anapitiriza kulambira monga mwa mofanana ndi kulambira kwa sunagoge. Akhristu a mitundu sakanakhala ndi chidziwitso cha miyambo ya Chiyuda mwina amapembedza mwa njira yosiyana. Ndi zachidziwikire, kuti, mpingo woyambirira unakhazikitsa chidwi chake pa malemba ndi kulalikira komanso kuphunzitsa Mawu a Mulungu.

---

30 1 Akorinto 14:16 akuchokera pa mchitidwe uwu.

31 Mateyu 28:18-20, Machitidwe 2:38-41, 1 Akorinto 11:20-34.

KULAMBIRA KWA BAIBULO LERO

Mu mipingo yambiri, kuwerenga kwa malemba pagulu kwachepekera. Sizachilendo kuona mipingo ya chivangeli imene mavesi ochepa amawerengedwa mu nthawi ya mwambo wa mapemphero. Malemba ayenera akhale poyambirira pa kulambira kwathu. Kudzera mu nyimbo zochokera mu Baibulo, kuwerenga Baibulo, kapena kugawa uthenga ozama mosamala mu ulaliki, tidzadziwika ngati "Anthu a Buku." Baibulo liyenera likhale ndi malo okhazikika mu kulambira kwathu.

FUFUZANI

Dzifunseni nokha, "Kodi kulambira kwanga kumakhala ndi zizindikiro za zimenne zinali mbali imodzi ya kulambira kwa mpingo woyambirira?"

CHIVUMBULUTSO: KULAMBIRA NGATI KULEMEKEZA

Kulambira ndi cholinga chachikulu cha Chivumbulutso.

- Yohane anali mu Mzimu patsiku la Ambuye panene anamva mawu akuti Alefa ndi Omega (Chivumbulutso 1:10).
- Chimodzi mwa zolinga zazikuluzukulu mu Chivumbulutso ndi kusiyanitsa pakati pa iwo amene amalambira Mulungu pampando wake wa chifumu ndi amene amalambira chilombo.

"Malizani tsopano chilengedwe chanu chatsopano,
Woyera ndi wopanda banga tikhale;
Tione chipulumutso chanu chachikulu chobwezeretsedwa bwino mwa Inu:
Kusinthika kuchoka mu ulemerero kupita mu ulemerero,
Kufikira kumwamba titenga malo athu,
Kuyimba ndi ndikuponya a korona athu pamaso panu.
Wodabwitsidwa, chikondi ndi matamando!"

Charles Wesley

- Chivumbulutso amalonjeza kuti Mulungu adzagonjetsa adani ake, ndipo mitundu yonse idzabwera ndi kumulambiraIye (Chivumbulutso 15:4).

Kuti timvetse kulambira mu Chivumbulutso, ndizothandiza kubwereza kuona ndondomeko ya mbiri yakale ya buku. Akhristu a zaka zana zoyambirira anatsutsidwa ndi zinthu ziwiri zopikisana. Mwanjira ina, anadziwa kuti Yesu ndi Ambuye (Afilipi 2:11). Chikhulupiriro mwa Yesu chimafuna kudzipereka ku ulamuliro ndi ukulu wa Yesu Khristu. Mbali ina Roma amafuna kuti aliyense wokhala pansi pa ulamuliro wa umfumu wawo kuti achitire umboni kuti Kaisara ndi mbuye ndi mulungu.

Sizinali zotheka kwa Akhristu kuti apereke ulemu waukulu kwa wina aliyense kupatula Mulungu. Chiyambi cha mkangano pakati pa Akhristu a zaka zana zoyambirira ndi Roma chinali, "Ndi ndani ofunika kulambira?" Mu ndondomeko iyi, Chivumbulutso amati "Yesu ndi Ambuye." Ndi woyenera kulambira. Chivumbulutso amapereka chithunzi cha kulambira koona.

Kulambira kwa Kumwamba kunasiyanitsidwa ndi kulambira kolephera

Chivumbulutso amayamba ndi mauthenga opita ku Asiya. Asiya anali m'modzi mwa madera a mphamvu amene kumachitika chipembedzo chopembedza mafumu. Kunali makachisi amene analembedwera mu Chivumbulutso. Kulambira kwa mafumu kunali komvomerezeka mudera lonse.

Uthenga wa ku mipingo isanu ndi iwiri ukuonetsa kulephera mu kulambira kwa mipingo yambiri. Pamene mipingo isanu ndi iwiri yonse ikulambira Mulungu, isanu mwa mipingoyi ikulandira chenjezo. Machenjezo akuonetsa kuti mipingo iyi inalephera kulambira Mulungu momvomerezeka.

1. **Kusoweka chikondi kumapondereza kulambira kowona.** Aefeso anachita bwino zinthu zambiri, koma anataya chikondi chawo cha poyamba. Kusamva kanthu pa kulambira chikhoza kukhala chizindikiro chakuti tataya chikondi chathu pa Mulungu amene timamulambira.

2. **Chiphunzitso chabodza chimapondereza kulambira kowona.** Peganamu ndi Tiyatira anamvomereza ziphunzitso zabodza. Kuopsa uku kukhoza kuoneka m'mipingo imene imasinthanitsa zizindikiro ndi zozizwa ndi choonadi cha Baibulo.

3. **Ntchito zakufa zimapondereza kulambira koona.** Mzinda wa Saridisi unagonjetsedwa kawiri pamene alonda ogona analephera kuona kuyandikira kwa mdani.[32] Yohane anachenjeza kuti mpingo wa Saridisi unali wogona chifukwa

32 Izi zinachitika pamene Kirusi anagwidwa mu 547 B.C. komanso pamene Antiokasi III anagwidwa mu 214 B.C.

unakhulupirira mu ntchito zake zabwino. Kukumana ndi Mulungu pa kulambira kukanadzutsa Saridisi ku tulo take.

4. **Kusoweka kukhudzika kumapondereza kulambira kowona.** Laodekiya anaonetsa mzimu wa kufunda umene mpingo unakhala ukuona mu nthawi ya kulemera. Kusoweka kwa kukhudzika kwa anthu a ku Laodekiya kunalimbikitsidwa ndi chuma chawo komanso kukwanira pawokha. Kulambira kumatikumbutsa kudalira kwathu pa Mulungu.

Kulambira Kwa Kumwamba Kumalunjika pa Mulungu

Chivumbulutso 4-5 amaonetsa kuti kulambira kwa kumwamba kumalunjika kwa Mulungu komanso ulemerero wake. Wolambira a kumwamba amalambira Mfumu Yamuyaya komaanso Yowuka kwa akufa.

Kodi mungafanizire mngelo akunena kwa Yohane, “Kodi chilipo china chilichonse chimene tingasinthe kukupangitsani inu kuti mumve bwino pa kulambira?” Zachidziwikire ayi! Kulambira ndi kwa Mulungu, osati kwa ine. Kulambira kumadalitsa wolambira koma chimenecho sicholinga choyambirira cha kulambira. Cholinga cha kulambira ndi kulemekeza Mulungu. Wolambira ozungulira mpando wa chifumu wa Mulungu amayimba nyimbo ya matamando kwa Mulungu:

> Iwo ankayimba nyimbo ya Mose, mtumiki wa Mulungu, ndi nyimbo ya Mwana Wankhosa. Nyimbo yake inkati, “Zochita zanu ndi zazikulu ndi zodabwitsa, Ambuye Mulungu Wamphamvuzonse Njira zanu ndi zachilungamo ndi zoona, Mfumu ya mitundu yonse. Inu Ambuye, ndani angapande kukuopani, ndi kulemekeza dzina lanu? Pakuti Inu nokha ndiye woyera. Anthu a mitundu yonse adzabwera kudzapembedza pamaso panu, pakuti ntchito zanu zolungama zaonekera poyera” (Chivumbulutso 15:3-4).

Kulambira kwa kumwamba kumachitika mkupezeka kwa Mulungu. Kuyambira pa nthawi imene Adamu ndi Hava anatulutsidwa m’munda, munthu wakhala osiyanitsidwa kwa Mulungu. Kumwamba, kulambira kudzachitikanso m’kupezeka kwa Mulungu zotchinga zina zilizonse zochokera kwa woipa.

> Ndipo ndinamva mawu ofuwula kuchokera ku Mpando Waufumu kuti, “Taonani! Malo wokhalapo Mulungu ali pakati pa anthu, ndipo Iye adzakhala ndi anthuwo. Iwo adzakhala anthu ake ndipo Mulungu mwini adzakhala nawo nakhala Mulungu wawo” (Chivumbulutso 21:3).

Kulambira kwa Kumwamba Kumaonetsera Zoona Zenizeni

Pamene amalemba Chivumbulutso, Yohane anali m'ndende pa chilumba cha Patimo. Akhristu mu ufumu wa Roma onse anali muchizunzo. M'maonedwe a dziko, tsogolo linali lakuda. Koma, Chivumbulutso amaonetsa masomphenya a kumwamba pazochitika za padziko.[33]

Padziko, timaona mbali imodzi ya mbiri. Timayesedwa kuganiza kuti dziko lotizungulira ndi zenizeni. Kumwamba ndi kulambira zimaoneka zochotsedwa ku zovuta za dziko lenileni. Zooneka zochepa za kulambira kwa kumwamba zooneka pa Chivumbulutso 4, 5, ndi 15 zimationetsa chithunzi cha dziko lenileni.

Kwa ogwira ntchito a Chikhristu, Chivumbulutso ndi chikumbutso chofunikira kuti zovuta za dziko lino ndi zosakhalitsa. Kulambira sikuthawa kwa sabata ndi sabata ku zenizeni koma kulambira kumaonetsa zoona zenizeni kuchokera ku maonedwe a Mulungu – ndipo izi zimasintha maonedwe athu a dziko lathu. Mu Chivumbulutso, Mulungu akuti, "Zinthu sizophweka ngati m'mene zimaonekera. Zinthu sizokanika, Satana sanapambane, zoipa sizinagonjetse. Onani kudzera pakhomo ndikupeza zoona zenizeni. Mulungu ali pampando wake."[34]

KULAMBIRA KWA BAIBULO LERO

"Wauka!" "Ndi Ambuye!" Zonenera izi ndi zofunikira ku kulambira. Ndi chiukitso chimene chinatsimikizira Yesu ngati Ambuye (Aroma 1:4).

Mpingo woyambirira unavomereza tsiku la Sabata lina lililonse ngati chikondwerero cha chiukitso; tsiku la Sabata lililonse linali Chiukitso. Akhristu sanali kusala pa tsiku la Sabata; tsiku la Sabata linali la chikondwerero.

Lero, kulambira kwathu kukhale nthawi ya chikondwero. Zoona, pali Mwambo wophatikizana ndi kulowa mkupezeka kwa wa M'mwamba, komanso pali kukondwerera pamene tikondwerera Ambuye woukitsidwa. Kulambira kwathu kukhale ndi mwayi wa chikondwerero.

Kulambira kumakhala ndi nyimbo za matamando komanso ma umboni a chisomo cha Mulungu m'miyoyo ya mamembala. Mpingo wa ku Nigeria umakondwera akamapereka chopereka. Mamembala amavina kuzungulira chopereka chikamatengedwa. Wolambira awa amadziwa chimwemwe cha chiukitso. Kulambira kuyenera kukhale ndi mwayi wokondwerera chigonjetso chimene tinachipeza kudzera mu chipambano cha Yesu pa imfa.

---

33 Mwachitsanzo: 6:1-7:8 zili padziko; 7:9-8:6 zili kumwamba. 8:7-11:14 zili padziko; 11:15-19 zili kumwamba.

34 David Jeremiah. *Worship*. (CA: Turning Point Outreach, 1995), 72.

FUFUZANI

Dzifunseni nokha, “Kodi kulambira kwanga ndi kukondwerera kapena ntchito? Kodi ndimakondwera kulowa mu kulambira, kapena ndimapita kolambira chifukwa chakuti ndi udindo wanga ngati M’khristu?”

CHITANI ZIMENEZI

Tengani nthawi yoganizira pa Mulungu amene timamulambira. Ganizirani za zimene malemba atiuza za Iye.

KODI MULUNGU NDI NDANI MU MALEMBA[35]	
Mu Genesis	Ndi Mlengi wa Dziko Lonse
Mu Eksodo	Mwanawankhosa Wakupulumutsa
Mu Levitiko	Ndi Nsembe ya Ngwiro
Numeri	Ndi Mtambo
Mu Deuteronomy	Ndi m'modzi mwa Aneneri Owona
Mu Yoswa	Ndi Woyang'anira wagulu la Nkhondo la Yehova
Mu Rute	Ndi Wowombola wa Abale
Mu 1 ndi 2 Samueli	Ndi Mneneri
Mu Mbiri	Ndi Kachisi wa Kumwamba
Mu Yobu	Ndi Mkhalapakati
Mu Masalimo	Ndi M'busa
Mu Yesaya	Ndi Karonga Wamtendere
Mu Ezekieli	Ndi Mwana wa Munthu
Mu Hoseya	Ndi Wochiritsa wa Obwerera M'mbuyo
Mu Haggai	Ndi Chokhumba cha a Mitundu
Mu Malaki	Ndi Dzuwa la Chilungamo
Mu Mateyu	Ndi Mesiya Wolonjezedwa
Mu Marko	Ndi Kapolo
Mu Luka	Ndi Mwana wa Munthu
Mu Yohane	Ndi Mawu
Mu Aroma	Ndi amene Amalungamitsa
Mu Afilipi	Ndi Chimwemwe Chathu
Mu Akolose	Iye ndi Chidzalo cha Umulungu
Mu Aheberi	Ndi Wansembe Wamkulu Woposa
Mu 1 ndi 2 Petro	Ndi M'busa wa Nkhosa
Mu Chivumbulutso	Ndi Mwana wa Nkhosa amene anaphedwa, Mfumu ya Mafumu, ndi Mfumu ya Mafumu!

35 Izi zatengedwa kuchokera mu Vernon Whaley, *Called to Worship.* (Nashville: Thomas Nelson, 2009), 331-333.

KUMALIZA: UMBONI WA MTUMWI YOHANE

“Dzina langa ndi Yohane. Moyo wanga wasinthika kudzera mu kulambira. Kuyambira pa nthawi yoyamba imene ndinakumana ndi Yesu wa ku Nazareti, ndakhala wolambira.

“Ndinalipo Paphiri la Kusandulikira Ophunzira atamva zimenezi, Ophunzira atamva zimenezi, anachita mantha nagwa pansi chafufumimba (Mateyu 17:6). Tinalambira mosayenera. Zochita zathu mu Sabata ya mazunzo zinaonetsera kuti sitinazindikire zimene tinaona Paphiri.

Atamuona Iye, anamulambira; koma ena anakayika (Mateyu 28:17). Tinalambira mosayenera. Tinadziwa kuti wauka, koma sitinazindikire zonse zimene zimatanthauza.

“Tinali m’chipinda chapamwamba pamene tinadzikhuthula tokha ku pemphero ndi mtima umodzi (Machitidwe 1:14). Pamene timalambira, Mzimu Woyera anatsikira pa ife. Kulambira kunakhala cholimbikitsa kufalitsa uthenga; tinapereka uthenga ku Yerusalemu, Yudeya ndi Samariya, ndikufikira malekezero a dziko lapansi.

Pa tsiku la Ambuye ndinanyamulidwa ndi Mzimu ndipo ndinamva kumbuyo kwanga mawu ofuwula ngati lipenga, amene anati, “Lemba m’buku zimene ukuziona ndipo uzitumize ku mipingo isanu ndi iwiri ya ku Efeso, Simurna, Pergamo, Tiyatira, Sarde, Filadefiya ndi ku Laodikaya” (Chivumbulutso 1:10-11).

“Ndinaliko pamene Mulungu anatsegula khomo la kumwamba ndikundilola kuti ndione kulambira kozungulira Mpando Wachifumu wa Mulungu.

“Ndinaona mzinda wopatulika, Yerusalemu watsopano, ukutsika kuchokera kumwamba kwa Mulungu, utakonzedwa ngati mkwatibwi wovala zokongola kukonzekera mwamuna wake (Chivumbulutso 21:2). Mu mzinda umenewo, kulambira kwathu kudzakhala kwabwino chifukwa tidzaona nkhope ya amene timamulambira. Kumwamba, Ndipo ndinamva mawu ofuwula kuchokera ku Mpando Waufumu kuti, “Taonani! Malo wokhalapo Mulungu ali pakati pa anthu, ndipo Iye adzakhala ndi anthuwo. Iwo adzakhala anthu ake ndipo Mulungu mwini adzakhala nawo nakhala Mulungu wawo” (Chivumbulutso 21:3).

“Ndine Yohane. Ndipo ndidzakhala kwa muyaya mu kulambira kwa Mulungu komanso Muwomboli!”

CHITANI ZIMENEZI

Musadamalize phunziro ili, khalani ndi nthawi ya kulambira. Werengani nyimbo za Chivumbulutso 4, 5 ndi 15 kapena Masalimo 19. Imbani nyimbo imene imalemekeza Mulungu. Pempherani pemphero la kulemekeza. Mvetserani pamene Mulungu akuyankhula kwa inu. Khalani ndi nthawi ya kulambira Mulungu.

KUKAMBIRANA KWA GULU

» Kuti mugwiritse ntchito bwino Phunziroli, kambiranani izi:

Tim amatumikira mpingo umene uli okhudzika ndi kafalitsa uthenga. Otembenuka mtima atsopano amabatizidwa sabata iliyonse. Ndi nthawi yosangalatsa mu mpingo.

Komabe, Tim ndiwokhudzika ndi kuti mpingo sukulambira moona. Ulaliki wambiri umalunjika kwa osakhulupirira komanso otembenuka mtima atsopano. Ndizovuta kugwiritsa ntchito zabwino chifukwa otembenuka mtima kumene sadziwa nyimbo. Tim akuopa kuti mpingo wake ukhala waukulu m'chiwerengero. Kambiranani zimene Tim angachite kuti kutsindikiza kwa kufalitsa Uthenga Wabwino kukhalepobe pamene akuzamitsanso kulambira kwa mpingo.

KUBWEREZA KUONANSO PHUNZIRO 4

1. Mabuku a Uthenga Wabwino amaonetsa kuti kulambira kumakwaniritsidwa mwa Yesu Khristu:

- Yesu anapereka chitsanzo cha kulambira.
- Yesu anakana yesero la kulambira kwabodza.
- Yesu anapereka chitsanzo chakufunikira kwa pemphero.
- Yesu adzalambiridwa kwa muyaya.

2. Machitidwe amaonetsa ubale wapakati pa kulambira ndi kulalikira.

- Kulambira koona kumalimbikitsa kufalitsa uthenga wabwino.
- Kufalitsa uthenga kwa mphamvu kumapanga wolambira.
- Kulambira kumene sikufikira ku kulalikira kudzakhala kodzikundikira.

3. Mabuku a Makalata amaonetsa zizindikiro zofunikira mu mpingo woyambirira. Kulambira mu mpingo woyambirira kunali ndi:

   - Kuwerenga Mawu
   - Kulalikira Mawu
   - Kupemphera pagulu
   - Kuyimba
   - Zopereka
   - Ubatizo
   - Mgonero wa Ambuye

4. Chivumbulutso amaonetsa kuti kulambira ndi kulemekeza Mulungu.

   - Kulambira kumadalitsa wolambira, koma chimenechi sicholinga choyambirira cha Kulambira.
   - Cholinga choyambirira ndikubweretsa ulemu kwa Mulungu.
   - Kulambira kumwamba kumatikumbutsa kuti dziko limene timaona sizazikulu zenizeni.

NTCHITO YA PHUNZIRO 4

1. Tchulani mfundo zitatu za kulambira kuchokera muphunziro ili. Pa mfundo iliyonse lembani ndime imodzi ya m'mene mungagwiritsire ntchito mfundo iyi mu mpingo mwanu.

2. Kumayambiriro kwa phunziro lotsatira, mudzalemba mayeso kuchokera pa phunziro ili.

MAYESO A PHUNZIRO 4

1. Tchulani njira zitatu zimene Yesu anaperekera zitsanzo za kulambira koona.
2. Kodi kuphunzitsa komanso chitsanzo cha Yesu zikutikumbutsa chiyani za kulambira koona?
3. Kodi ndi ziganizo ziwiri ziti zimene zikufotokozera ubale wa pakati pa kulambira koona ndi kulakira?
4. Kodi kulambira kwabodza kwa Atene kukufotokozeredwa motani pa Machitidwe 17?
5. Kodi Mulungu owona akufotokozeredwa motani pa Machitidwe 17?
6. Tchulani mfundo zisanu za kulambira koyambirira kwa Chikhristu mu mabuku a makalata.
7. Tchulani zitsanzo ziwiri za zotchinga kulambira zopezeka ku mipingo ya ku Ulaya.
8. Lembani Aroma 12:1-2 kuchokera pakuloweza.

PHUNZIRO 5

KULAMBIRA MU MBIRI YA MPINGO

ZOLINGA ZA PHUNZIRO

1. Kulemekeza kusiyana pakati pa miyambo ya chpempedzo zipembedzo yosiyanasiyana.
2. Kuzindikira kusiyana pakati pa mfundo zosasinthika za kulambira ndi miyambo yosinthika ya kulambira.
3. Kuzindikira kuti kulambira kumaonetsera zikhulupiriro zathu ndikupereka mphavu pa zikhulupirirozo.
4. Kutengapo maphunziro kuchokera pa miyambo ya kulambira ya mipingo yosiyanasiyana ndi kulambira kwa lero.

KUKONZEKERA PHUNZIRO ILI

Lowezani Masalimo 100:1-5.

CHIYAMBI

James amalemekeza kulambira kwa chikhalidwe. Pa mkumano wawo wa pamwezi Enoch, amene amatsogolera mwambo wa kulambira kwa makono, anafunsa, “Kodi ndi chifukwa chiyani simuyesa china chake chatsopano mu mwambo wanu wa mapemphero?”

“Ndife a Baibulo,” James anayankha. “Ngati Baibulo sililamula mwambo wina wake wa kulambira, sitili omasuka kungowonjezera ku miyambo ya kulambira ya mpingo woyambirira. Ndife ndani kuti tisinthe Kulambira kwa Baibulo? Mu mpingo wathu,

timayimba Masalimo okha. Nyimbo zimenezi zinali nyimbo za mpingo woyambirira; ndizokwanira kwa ife!"[36]

Enoch anayankha, "Zikumveka kwa ine ngati kuti mukuganiza kuti mbiri inathera kumapeto kwa buku la Chivumbulutso. Tingadziikire malire motere bwanji ku kalambiridwe kamene kali ndi zaka 2,000? Malingana ngati Baibulo sililetsa mwambo, komanso ngati mwambowo sugawanitsa mpingo, tiyenera kutengera kulambira ku zosowa za nthawi yathu. Mu mpingo wathu timayimba nyimbo zambiri zatsopano. Mulungu akanafuna kuti aletse nyimbo zatsopano, Baibulo likanaletsa momveka bwino."[37]

Yankho la Jason linali lothandiza. "Taphunzira zimene Baibulo limanena za kulambira. Timadziwa mfundo za kulambira kuchokera mmalemba. Tikuyenera kuwona m'mene Akhristu ena anazitengera mfundo izi mu m'badwo ulionse. Kodi kulambira kukuoneka motani mu mbiri ya mpingo?"

Jason akudziwa mfundo yofunikira pakufotozera kulambira. Ngakhale kuti mfundo za baibulo za kulambira ndi zosasintha, zochitika pa kulambira kulikonse mu Baibulo ndi zosiyana. Ndondomeko zimasiyana; zinthu zofunikira za kupembedza zimakhala chimodzimodzi. Taona mfundo zofunikira za kulambira m'maphunziro awiri apitawa, koma ndondomeko zimasintha. Lingalirani:

- Abrahamu anali pa hema wake pamene analambira. Ena akhoza kuwerenga izi ndikunena kuti, "Kulambira koona kumachitika ukakhala kunyumba." Koma…
- Yesaya anali mu Kachisi pamene anaona Yehova akukwezedwa. Ena akhoza kuwerenga izi ndikunena kuti "Kulambira koona kumachitika ukakhala ku tchalitchi." Koma…
- Yobu anali ndi zilonda kuyambira kumutu kufikira ku zala zakumwendo pamene anati "Ndinkangomva za Inu ndi makutu anga, koma tsopanonso ndakuonani ndi maso anga" (Yobu 42:5). Wina akhoza kurenga kuwerenga izi ndikunena kuti "Aha! Kulambira koona kumachitika ukakhala m'mavuto."

Kodi mukuona mfundo? Kulambira kumachitika mu nyengo zosiyasiyana, mu njira zosiyanasiyana, ndipo motsatira ndondomeko zambiri zosiyana. Nthawi zambiri timasokoneza nyengo zosinthika za kulambira ndi mfundo zosasinthika.

---

36 Iyi imatchedwa "mfundo ya lamulo" ya kulambira. Yophunzitsidwa ndi John Calvin, imakaniza machitidwe alionse amene sanakhazikitsidwe m'malemba. Pachiyambi, izi zinaletsa kugwiritsa ntchito zida zoyimbira (pakuti zida sizikutchulidwa mu kulambira kwa Chipangano Chatsopano) kapena kugwiritsa ntchito nyimbo zina zilizonse kupatula Masalimo. Mipingo ina imene imatsatira mfundo izi lero lino anawonjezera zida zoyimbira komanso nyimbo; koma amapitiriza kupewa njira zatsopano za kulambira.

37 Iyi imatchedwa "mfundo yokhazikika" ya kulambira. Ndondomeko iyi imaphunzitsa kuti machitidwe ena alionse a kulambira amene saletsedwa m'malemba ndi ololedwa, malingana ngati akusokoneza mtendere ndi umodzi wa mpingo.

Muphunziro ili tiona m'mene mpingo wagwiritsira ntchito izi za kulambira mu mbiri yonse. Izi zidzakupangitsani kuona njira zosiyasiyana zimene anthu a Mulungu amalambirira. Mwachiyembekezo izi zikuthandizani kuona kuti palibe ndondomeko ina iliyonse imene ikuyenera kutsatidwa ndi anthu onse m'nyengo zonse. Koma, tikuyenera kufunafuna chitsogozo cha Mzimu wa Mulungu kuti atitsimikizire m'mene tingagwiritsire ntchito mfundo za kulambira za Baibulo ku nyengo zathu.

Mu phunziro ili, tionanso kuti m'mene timalambirira zimaonetsa zikhulupiriro zathu. Ndondomeko zathu za kulambira zimachokera pa zikhulupiriro zathu pa Mulungu komanso m'mene timamufikirira.

Kumvetsetsa uku ndikovuta pamene mukupanga ziganizo za kulambira. Kodi mumachita mwambo wanu wa kulambira mu njira imene imaonetsera zikhulupiriro zanu, kapena mukutengera ndondomeko za mpingo wina? Ngati mukutengera mpingo wina, wonetsetsani kuti mukufanana ndi zikhulupiriro za mpingo umenewo pa za Mulungu komanso m'mene timamufikirira. Kulambira kwathu kumaonetsa zimene timakhulupirira.

» Tisanapitirize phunziro ili, kambiranani za mwambo wa kulambira kwanu pkadali pakadali pano. Ngati munthu sanadziwe kanthu za chiphunzitso chanu, kodi ndondomeko yanu ya kulambira idzanena chiyani kwa iwo? Kodi iwo aphunzira chiyani za mawonedwe a Mulungu?, mawonedwe anu a ubale wathu kwa Mulungu, komanso kuona kwanu kwa ulaliki ngati zotsatira za mwambo wanu wa kulambira?

CHITHUZI CHA KULAMBIRA MU ZAKA ZANA ZACHIWIRI

Chithunzi chathu choyambirira kwambiri cha kulambira pambuyo pa Chipangano Chatsopano chikuchokera mu kalata ya chaka cha A.D.113. Pliny, nduna ya ku Bitenia, anafotokozera kulambira kwa Chikhristu mu kalata yake yopita kwa Mfumu Trajan.[38] Analemba kuti Akhristu "amasonkhana pa tsiku limene lanenedwa m'bandakucha usanafike ndikuimba nyimbo kwa Khristu ngati kwa mulungu, ndipo amatenga lumbiro ...la kusaba, kusachita katangale wa ndalama, osachita chiwerewere... ndi Ndi mwambo wawo wakusiyana ndi kubwereranso kudzadya chakudya limodzi."

Monga mwa Pliny, Akhristu amakumana dzuwa lisanatuluke pa tsiku la Sabata ndi kuimba nyimbo zolonjeza kudzipereka ku khalidwe loyenera, mkutheka ndi kuvomera ku kuwerenga kwa malemba. Pamapeto pa tsiku limenelo, amadya chakudya, chimene mwina amaphatikiza ndi Mgonero wa Ambuye.

38 Pliny, *Letters 10.96-97*, Zotengedwa kuchokera https://faculty.georgetown.edu/jod/texts/pliny.html on January 26, 2023.

Patatha zaka makumi anayi, Justin Martyr anapereka ndondomeko yozama ya kufotokonzera kulambira.[39] Justin analemba kuyikira kumbuyo kulambira kwa Chikhristu kwa wolamulira Roma amene anaganizira Akhristu kuti anali osakhulupirika ndi osamvera kwa mfumu. Justin anatsimikizira mfumu kuti kulambira kwa Chikhristu sichinali chiopsezo ko Roma. Molingana ndi Justin, Kulambira kwa Chikhristu kunali ndi zinthu izi:

1. **Kuwerenga kwa Mawu.**

2. **Uthenga wolalikidwa ndi mtsogoleri wa gulu.**

3. **Pemphero.** Anthu amapemphera mwakachetechete; kenaka mtsogoleri amatsogolera pemphero la onse, limene anthu amayankha kuti, "Amen." Pamapeto pa pemphero, wolambira amapatsana moni wa mpsopsono wina ndi mzake kuwonetsa kupezeka kwa Mzimu Woyera.

4. **Mwambo unathera ndi Chiyanjano cha Mgonero.** Atamaliza mapemphero, atumiki awiri anatengera mkate ndi vinyo wotsala kwa Akhristu amene amadwala kapena amene anali mu ndende kudikira kuphedwa.

5. **Pamapeto pa mapemphero, amene anali ndi ndalama kapena anali ndi chakudya anabweretsa mphatso zawo kwa mtsogoleri.** Zopereka zimapitisidwa kwa "ana ndi amayi amasiye, amene ali ndi zosowa chifukwa cha matenda kapena zifukwa zina, komanso akapolo ndi alendo pakati pathu."

Chimodzi mwa zilimbiko za kulambira mu mpingo wa zaka zana zachiwiri kunali kutengapo mbali kwa anthu. Onse awiri Pliny ndi Justin Martryr anafotokozera mwambo osavuta, osakhala ndi miyambo yazochitika zambiri za mzipembedzo za mafano za ku Roma. Kulambira kunali kogwirizana, pamene magulu ang'onoang'ono anakumana m'nyumba zawo.

Chilimbiko china chinali mgwirizano pakati pa kulambira ndi moyo. Kalata ya Pliny ikunena za kudzipereka kwa Akhristu ku makhalidwe oyenera; Justin Martyr akunena za mphatso zothandizira osowa. Kulambira kunakhudza zonse zokhudza moyo.

» Kodi ndi mfundo ziti zakulambira za mu zaka zana zachiwiri zimene zingapindulire kulambira kwanu? Kodi mukuona zoopsa zina zilizonse mu kulambira kwa zaka za mazana awiri?

39 Justin Martyr, (Zotanthauziridwa ndi Marcus Dods), *The First Apology of Justin* (Chapter 67). Zatengedwa kuchokera https://en.wikisource.org/wiki/Ante-Nicene_Christian_Library/The_First_Apology_of_Justin_Martyr#Chapter_67 on January 26, 2023.

CHITHUNZI CHA KULAMBIRA MU ZAKA ZA PAKATIKATI

Kuti muone chithunzi chachiwiri cha kulambira, pitani ku zaka za mazana 12. Mu zaka za kulowerera, Chikhristu chinakhala chipembedzo cha Umfumu Woyera wa Roma. Utatha ulamuliro wa Constantine *wa Milan* mu zaka za A.D. 313, mipingo inayamba kumanga matchalichi akuluakulu. Ambiri mwa makachisi akuluakulu a ku maiko a ku Ulaya anamangidwa mu nthawi ya zaka 1000.

Mu zaka za pakatikati, kulambira kunakulirakulira. Mwakuchitira ubwino, kulambira kwa m'makachisi akuluakulu kunawonetsera ukulu wa Mulungu. Mazenera a dzimbiri anawonetsa nthawi ya zochitika za Baibulo kwa iwo amene sanali kutha kuwerenga. Makwaya anayimba nyimbo zabwino. Kulambira kunali kopatsa chidwi ndi kokongola.

Zofooka za Kulambira mu Zaka za Pakatikati

Kukongola kunali kofunikira kuposa uzimu.

Kugwiritsa ntchito zinthu zokongola pa kulambira zinatsindikizidwa: zonunkhiritsa, nyimbo zolongosoka bwino zoyimbidwa ndi oyimba ophunzitsidwa bwino, mabelu, ndi mavalidwe apaderadera a ansembe. Luso linasanduka lofunikira kuposa za uzimu.

Anthu samatha kuzindikira kutumikira.

Mapemphero anali kuchitika mu Chilatin Ansembe ambiri a komweko anali osaphunzitsika bwino kulalilira uthenga. Mapemphero anali zidutswa za ndime zochokera kosiyana ndipo samamveka mwanzeru.

Anthu anali oyang'anira, osati wolambira.

Panali kutengapo mbali kochepa kwa anthu. Mpingo unali gulu la owonerera sewero, misa. Ansembe amachita mwambo wa kulambira anthu amaonerera.chidwi cha mapemphero chinali Mgonero osati malemba.

Mpingo wa Chikalolika anaphunzitsa kuti mkate komanso vinyo zinali kusandulikadi kukhala thupi ndi mwazi wa Khristu (Ichi chimatchedwa chiphunzitso cha *kusandulika*). Anthu ambiri amalandira mgonero pa nthawi ya Kukumbukira kufa ndi kuukanso kwa akufa kwa Khristu. Wa nsembe amamwa vinyo ndi kugawana mkate wokha ndi gulu lonse.

Uthenga wabwino unalowedwa m'malo ndi mwambo.

Kulambira kwathu kumasula zikhulupiriro zathu. Tikuona mfundo iyi ikugwira ntchito mu Zaka za Pakatikati; Kulambira kwa Katolika kunapanga chiphunzitso chawo. Mulungu amaoneka kuti wachotsedwamo mu zofuna za anthu. Anthu wamba sanamve kuti akhoza

kufikira Mulungu; mmalo mwake amayankhula ndi Mulungu kudzera mwa wansembe. Wansembe anasanduka mkhalapakati wa pakati pa Mulungu ndi munthu.

Mphamvu ya kulambira mu Zaka za Pakatikati zinali maonekedwe ake a ukulu komanso kudabwitsa pamaso pa Mulungu. Kudzera muluso lomanga, kulambira kunawonetsera ulemerero wa Mulungu.

Komabe, zofooka za kulambira mu Zaka za pakatikati zinachuluka kuposa zilimbiko zake. Akhristu Wamba anali owonerera mwambo wa kulambira. Munjira zambiri, kulambira kwa Zaka Za pakatikati kunali kutuluka koopsa kuchokera mu kulambira kwa Chipangano Chatsopano.

ZIOPSEZO ZA KULAMBIRA: KULAMBIRA KOPANDA TANTHAUZO

Tiyenera kutenga nthawi kuphunzitsa mpingo wathu kuti ndi chifukwa chiyani timalambira m'mene timachitira, kupatula apo miyambo yatanthauzo ikhoza kuoneka yopanda tanthauzo kwa wolambira.

Okhulupirira watsopano anafunsa abusa ake, "kodi ndi chifukwa chiyani timati 'Amen' kumapeto kwa mapemphero? Kodi 'Amen' ndi liwu la mphamvu limene limapangitsa Mulungu kuchita monga tafunsa?" Abusa anazindikira kuti ayenera kufotokoza ndondomeko za kulambira. China chake chosavuta monga "Amen" chikhoza kukhala chopanda tanthauzo ngati sitiphunzitsa mpingo wathu za kulambira.

Sizofunikira kuchotsa chizindikiro komanso chinsinsi cha kulambira. Kuthana ndi vuto ndi kuphunzitsa tanthauzo la machitidwe a kulambira kwathu. Adziwe chifukwa chimene timagwiritsa ntchito chiyankhulo chimene timagwiritsa ntchito; adziwe kuti kuyimba kwa mpingo onse ndikofunikira ku mpingo; adziwe zimene malemba amatanthauza.

» Kodi ndi mfundo ziti za kulambira mu Zaka za Pakatikati zimene zingapindulire kulambira kwanu? Kodi mukuona ziopsezo zina zilizonse mu kulambira kwa Zaka za Pakatikati?

CHITHUNZI CHA KULAMBIRA MU NTHAWI YA KUKONZANSO

Anthu okonzanso zinthu anadziwa bwino kuti kulambira kwathu kumasula chikhulupiriro chathu.chifukwa cha ichi, anadziwa kuti zoonadi za chikhupiriro cha Kukonzanso chidzataika pokhapo ngati kulambira kumaonetsera chikhulupiriro cha umulungu.

Cholinga chachikulu cha okozanso chinali unsembe wa okhulupirira. Izi zitanthauza kuti okhulupirira amalambira Mulungu molunjika; sadzeranso mwa wa nsembe. Okozanso zinthu anakhupirira kuti Mawu a Mulungu ayenera akhale opezeka kwa okhulupirira aliyense.

Kulambira mu nthawi ya kukozanso kunafuna kuti okhulupirira aliyense atengepo mbali. Kulambira kunali mu chiyankhulo cha anthu, osati Latin. Malemba amawerengedwa ndi kularikidwa kuti wolambira amve Mawu a Mulungu mu chiyankhulo chawo. Nyimbo za mpingo onse zinapangitsa wolambira aliyense kutengapo mbali pa kulambira. Martin Luther anali wolemba nyimbo, ndipo nyimbo zake zimapatsidwa ulemu pa kuthandiza kafalikira kwa Kukonzanso.

Kupitirira madera odziwika bwinowa, panali kusagwirizana kwakukulu pakati pa Wokozanso zokhudza kulambira. A Lutheran ndi Anglican anasunga yambiri ya miyambo mwa mpingo wa Katotika. Luther anakhulupirira kuti, kupatula pokhapo ngati zinakanizidwa mu Baibulo kapena kuyambitsa mikangano mumpingo, miyambo yolambira yatsopano iyenera kuloledwa mumpingo.

Calvin anali ndi omutsatira anakhazikika pa miyambo ina koma anakana miyambo ya kulambira imene sinakambidwe m'malemba. Calvin analimbikitsa kuyimba kwa mpingo onse, koma kwa Masalimo okha. Anakhulupirira kuti "Mawu a Mulungu okha ndi amene ali oyenera kuyimba mu matamando a Mulungu."[40] Anapitanso pa kutengapo mbali kwa Mgonero, pakupereka maganizo akuti Mgonero wa Ambuye uzidyedwa pafupifupi kamodzi pamwezi kapenanso pa Tsiku la Ambuye.

Ma Anabaptist ndi a Puritan anakana miyambo yambiri ndikupita ku kulambira mwanjira yosavuta. Magulu amenewa nthawi zina analambira m'nyumba zawo ndikudziona okha ngati okhawo amene anatsatira kulambira kwa zaka za zana limodzi.

Chilimbiko cha kulambira kwa Kukonza kunali kubwereranso ku kutengapo mbali kwa gulu. Ngakhale panali kusiyana pakati pa mipingo yosiyanasiyana pa za Kukonzanso, onse obweretsa Kukonzanso anafuna kubweretsa chitsanzo cha unsembe wa okhulupirira mu Kulambira.

» Kodi ndi maganizo otani mu kukozanso amene angapindulire kulambira kwanu? Kodi mukuona zoopsa zina zilizonse mu kulambira kwa Kukonzanso?

CHITHUNZI CHA KULAMBIRA MU M'MIPINGO YA UFULU

Kutsatira kukozanso, mipingo ina inakana ulamuliro wa dziko. Mipingo imeneyi yotchedwa "mipingo ya ufulu" munali Anabaptist, a Puritan, Noncormformists, Separitists ndi ma Dissenters. Ambiri mwa awa anakana mapemphero ndi miyambo yokhazikitsidwiratu.

Zooneka za kulambira kwa mpingo wa ufulu:

40 Zatengedwa mu Donald P. Hustad, Jubilate II (Carol Stream: Hope Publishing Company, 1993), 194.

1. **Kulalikira kunali cholinga chachikulu.**

2. **Kutengapo mbali kwa gulu kunali kofunikira.**

Kutengapo mbali kwa gulu kunali kosiyana pakati pa mpingo ndi mpingo.

- M'mipingo ina gulu limayimba nyimbo. M'mipingo ina, kunalibe nyimbo mukulambira kwa pagulu.
- M'mipingo ina mamembala a mpingo amapemphera mokweza. M'mipingo ina m'busa amapemphera m'malo mwa anthu.

Panali kusiyana pang'ono pakati pa umembala ndi ubusa. Mipingo yambiri ya ufulu inalibe zovala zapaderadera za ubusa.

3. **Mwambo onse wa kulambira unali muchiyankhulo cha anthu.**

Ndondomeko ya mwambo wa mapemphero mu 1608 uli ndi izi (mwambo umatenga ma ola anayi):

- Pemphero
- Kuwerenga malemba (machaputala awiri kapena atatu kuphatizapo kumasulira kwake)
- Pemphero
- Uthenga (wa ola limodzi kapena kupitirira)
- Zoyankhula za anthu
- Pemphero
- Chopereka

Kulambira sikumalandidwanso malo ndi mgonero ndi wa nsembe. Kulambira kwa mipingo ya ufulu kunaoneka mofanana kwambiri ndi kulambira kwa Chipangano Chatsopano.

Pali chiopsezo pa kufikira pa kulambira uku. Ngakhale mipingo ya ufulu inaphunzitsa za unsembe wa okhulupirira, pakuchita mwambo mlaliki nthawi zina amatenga malo a wansembe ngati chindunji cha kulambira. M'mipingo ina, munali kutengapo mbali kwa gulu kochepa.

Mwina chimodzi mwa zoopsa kwambiri za kulambira kwa ufulu kunali kudutsa mulingo kwa kuchita zinthu kwa munthu kodziimira payekha. Ngati chiphunzitso cha unsembe wa okhulupirira sichiyendera pamodzi ndi chiphunzitso cha umodzi wa mpingo, mpingo umasanduka msonkhano wa anthu odziimira pawokha osati thupi la Khristu loyanjanitsidwa mu kulambira. Izi zimaoneka pamene kulambira kuli kwa "Yesu ndi ine" popanda china chilichonse cha mpingo ngati thupi.

» Kodi ndi mfundo zotani za kulambira kwa mu mipingo ya ufulu zimene zingapindulire kulambira kwanu? Kodi mukuona zoopsa zina mu kulambira kochitika mu mipingo ya ufulu?

CHITHUNZI CHA KULAMBIRA MU CHITSITSIMUTSO CHA WESLEY

John Wesley anakhudzika kwambiri ndi kulambira kwa gulu kumene analandira kuchokera ku mpingo wa Anglican ndi kutsimikizika kwa uzimu wa payekha umene analandira kudzera mu kulumikizana ndi mwambo wa Anabaptist. Munthawi imeneyo pamene kulambira kwa Anglican kumatsatira kumambira kwa Mpingo wa Katolika kukhala mwambo opanda kanthu, a Wesley ndi otsatira awo (otchedwa a Methodist) anatsitsimutsa zoona zenizeni za kulambira zimene zinabweretsa olambira mu kupezeka kwa Mulungu.

Zotsindika za kulambira kwa Methdist koyambirira:

1. **Ulaliki.** Maulaliki a John Wesley amasindikizidwa ndipo anakhala maziko a chiphunzitso cha wolambira a Methodist.

2. **Mgonero wa pafupipafupi.** John Wesley analandira mgonero pafupifupi maulendo asanu pasabata. Analimbikitsa omutsatira ake kulandira mgonero pafupifupi kamodzi pa sabata.

3. **Kuyimba.** Nyimbo za Charles Wesley zinafalitsa chiphunzitso cha Methodist kudzera mu mipingo ya ku Britain ndi ku Dziko Latsopano.

4. **Magulu a anthu ochepa.** Mikumano inali chinthu chofunikira kwambiri pa kupanga ophunzira a Methodist.

Methodist ndi Kulambira kwa zaka za mazana Khumi zisanu ndi zitatu

Methodist anadzuka pakuona zolephera mu kulambira kwa mu zaka za m'mazana khumi zisanu ndi zitatu (1800)

"Pamene miyambo inali kumbali kwa moyo wampingo, methodist oyambirira anaika pakati; pamene changu cha chipembedzo chinali posokonekera, Methodist anachita zothekera; pamene chipempedzo chinabisika mu m'mipingo, Methodist anapititsa m'madera ndi m'makwalala."

James White in Robert Webber

Zaka za mazana makumi awiri za Kulambira kwa Chikhristu

5. **Kulambira kwa pamodzi.** A Methodist anali kukumana pafupipafupi, ngakhale pamene ansembe ambiri a Anglican anakana a Methodist, Wesley analimbikitsa omutsatira ake kupita ku mapemphero a Anglican.

6. **Chisokole.** Zikwizikwi za anthu otembenuka atsopano zinabwera kwa Khristu pamene chitsitsimutso cha Methodist chinafalikira ku England ndi madera ena.

Kulambira kwa Methodist kunali ndi nyimbo zimene zinalemekeza Mulungu, kupanga ophunzira kumene kunapanga ophunzira okula, komanso kulalikira kumene kunalengeza choonadi ku mpingo komanso ku dziko losoweka.

» Kodi ndi mfundo ziti za kulambira mu chitsitsimutso cha Wesley zimene zingapindulire kulambira kwanu? Kodi mukuona zoopsa zina zilizonse mu kulambira kwa chitsitsimutso cha Wesley?

CHITHUNZI CHA KULAMBIRA MU AMERICA WOYAMBIRIRA

Anthu a Chingelezi poyambirira anakhala kum'mawa kwa Gombe la malo amene tsopano amatchedwa United States of America. Munthawi ya kumapeto kwa zaka za 1700 ndikupitirirapo, anthu anapitiriza kupita kumadzulo kwa madera opanda anthu kuti akapeze malo ndi kumangako nyumba. Anthu anakumana ndi zovuta zambiri pamene mipingo, masukulu, komanso kukhazikitsa kwa lamulo zinakhazikika mochedwa. Mu mbiri dera ili limene linakhazikika pang'onopang'ono limatchedwa malire a chigawo cha America.

Cholinga chophunzirira kulambira mu mbiri yoyambirira ya America sikufuna kukhazikitsa America ngati chitsanzo cha kulambira konse, koma kufanizira ndi kulambira kumene kumakhazikitsidwa m'mipingo ing'onoing'ono m'madera ena. Mavuto oterewanso amapezeka ndi mipingo yokhazikitsidwa kumene m'maiko ambiri.

Zopezeka mu kulambira mu America woyambirira:

1. **Ufulu wa kusakha kukhala mu mpingo wina uli onse komanso machitidwe okhazikika a kulambira.** Mipingo yokhala ndi malire ya America inali yosamangika ku ulamuliro wa mpingo wina ulionse. Unapereka chidwi chochepa ku miyambo ndi ndondomeko zokhazikika za kulambira (ngakhale kuti John Wesley anatengera ndondomeko zake za kulambira kuti agwiritse ntchito m'madera). Zimango za tchalitchi ndi mwambo wa kulambira zinali zosavuta koma zoveka mophweka.

2. **Mwayi wapatalipatali wa Mgonero.** Ku England, a Wesley analimbikitsa kufunikira kwa mgonero kwa pafupipafupi. M'malire a America, kusoweka kwa abusa oyenerezedwa kunatanthauza kuti okhulupirira anali ndi mwayi wochepa wochita Mgonero wa Ambuye.

3. **Kulalikira kwa Mawu.** Kulalikira kunapitirira kukhala cholinga choyambirira pa mwambo wamapemphero. Ngakhale alaliki osaphuzitsidwa osaphunzitsidwa amawerenga mauthenga a Wesley ndi atumiki ena. Cholinga chachikulu chinali ulaliki osati gome la Mgonero. Cholinga chachikulu chinali kulalikira kwa Mawu.

4. **Kuyimba mwamphamvu.** Kuyimba kunali kwa mphamvu. Mipingo ya ku America inayimba nyimbo za Charles Wesley pambali pa nyimbo zina zosavuta za umboni munjira imene inali yosavuta ku mpingo wa anthu osaphunzira kuti athe kuphunzira.

5. **Pemphero, chisokole, ndi chitsitsimutso.** Pemphero linali losachita kuika ndondomeko ndipo nthawi zambiri limatsogozedwa ndi munthu wamba. Chisokole chinali chofunikira, ndipo nthawi zambiri za chitsitsimutso America anawona kutembenuka mtima kwa zikwizikwi. Uthenga umatsatirana ndi kuitana anthu osatembenuka mtima kuti abwere kutsogolo ndi kupemphera pemphero la kulapa. Pamene kutsindika kwa chiyero cha Chikhristu kunafalikira kwa America, kuitana kunabweretsa anthu kukutembenuka kukutembenuka ndi okhulpirira kudzamalizitsa ndondomeko yoyeretsedwa.

Monga mwa miyambo ina, munalinso zilimbiko ndi zifooko mu kulambira uku. Zilimbiko zinali za kutengapo mbali komanso kukhudzika kwa munthu payekha. Zoopsa zinali za munthu kukhazikika payekha ndikukhala ndi kukhazikika pang'óno mu chiphunzitso. Zinali zosavuta kuti chiphunzitso chabodza chifalikire m'malire a zigawo chifukwa panali umwini ochepa.

» Kodi ndi mfundo ziti za kulambira kwa malire a chigawo cha America chimene chingapindulire kulambira kwanu? Kodi mukuona zoopsa zina zilizonse mu kulambira kwa malire a zigawo za mpingo wa America?

ZOOPSA ZA KULAMBIRA: KUSOKONEZA MIYAMBO YOSINTHIKA NDI MFUNDO ZOSASINTHIKA

Nthawi zambiri timayesedwa kusokoneza miyambo yosinthika ya kulambira ndi mfundo zosasinthika za kulambira kosavuta. Ganizirani:

- M'mipingo ina, olambira amaima, amagwada pa maondo awo kuonetsa kudzichepetsa akamapemphera. M'mipingo ina wolambira amakweza manja awo oyera akamapemphera.
- M'mipingo ina, zida zimaimbidwa mwakayaziyazi mu nthawi ya pemphero. M'mipingo ina, pamakhala bata abusa akamatsogolera pemphero. M'mipingo ina, aliyense amapemphera mokweza.
- M'mipingo ina, makolasi amaikidwa ndi kumaoneka kutsogolo pa nsaru ya kanema. M'mipingo ina, anthu amaimba akuyang'ana mu buku la nyimbo.

- M'mipingo ina, abusa amawerenga malema pachiyambi pa uthenga waawowawo. M'mipingo ina, munthu wamba amawerenga malemba abusa asanalalikire. M'mipingo inu muli kuwerenga kwa mawu kawiri kapena katatu.

Onse mwa awa palibe amene akulakwa; ndi mwambo chabe, osati mfundo. Tisamaganize kuti njira yathu ndiyo njra ya Baibulo. Kulambira koona si machitidwe; koma ndi kupezeka kwa Mulungu.

Pali mfundo zina zimene zili zosasinthika. Tinaona mfundo zimenezi mu maphunziro a kulambira mu Baibulo. Mfundo izi sizochita kusankha. Ngati a Khristu, mfundo izi zimatitsogolera mukufikira kwathu kwa Mulungu.

Mumaphunziro ochepa amene akubwerawa, tiona pa miyambo ya kulambira. Mfundo sizisintha; miyambo imasiyanasiyana m'malo osiyanasiyana komanso nthawi. Chifukwa cha ichi, tiyenera kukhala ololerana ndi iwo amene amapembedza mosiyana ndi m'mene ife timachitira. Izi sizikutanthauza kuti mwambo siyofunikira; koma zikutanthauza kuti padzakhala kulolera kwakukulu pa kusiyana miyambo ndi mfundo.

Oswald Chambers analemba zopanga malo a Mulungu m'miyoyo yathu izinso zikugwirizana ndi kulambira:

> Ngati atumiki a Mulungu, tiyenera kupereka mpata ya kwa Iye… Timakonzekera, koma timaiwala kupereka mpata kwa Mulungu kuti abwere m'mene Wafunira. Kodi tikhoza kudabwa titaona Mulungu atabwera mumkumano wathu munjira imene sitinayembekezere Iye kubwera? Musayembekezere Mulungu kubwera mwanjira ina yake, koma mufuneni. Njira yoperekera mpata kwa Iye ndikuyembekezera Iye kubwera, chitani mwa njira ina yake…
>
> Pangani moyo wanu kukhala olumikizana ndi Mulungu nthawi zonse kuti mphamvu yake yodabwitsa ikhoza kubwera nthawi ina iliyonse. Khalani ndi chiyembekezo nthawi zonse, ndikupereka mpata kuti Mulungu abwere m'mene afunira.[41]

KUMALIZA: CHITHUNZI CHA KULAMBIRA LERO

Kodi kulambira kumaoneka motani mu zaka za mazama 21? Ndi funso limene silingayankhidwe mosavuta. Kulambira mu zaka za zana 21 kuli ndi machitidwe ambiri osiyana. Mipingo ina imalemekeza miyambo ndi chikhalidwe; mipingo ina imakana miyambo pofuna kulemekeza ufulu wa munthu wa kulambira.

M'malo mowona kufotokozera kwa kulambira lero, Tengani nthawi yopanga kufotokozera kwanu. Kodi kulambira kumaoneka motani mu mpingo mwanu? Ngati mukuphunzira pa

41 Oswald Chambers, *My Utmost for His Highest* (January 25 entry). Retrieved from https://utmost.org/leave-room-for-god/ on July 22, 2020.

gulu, kambiranani, kufanana ndi kusiyana kwa pakati pa kulambira mu mpingo kumene kwaperekdwa kwaperekedwa pa gulu.

Pa nthawi ino ya phunziro, cholinga cha kufotokozera uku sikupereka chigamulo. Funso si, "Kodi tikukhoza kapena tikulakwitsa?" Funso ndilakuti, "Kodi timachita chiyani mu mwambo wathu wa kulambira?"

Cholinga cha kufotokozera uku ndikuika maziko a maphunziro otsatira. Mukakhala ndi kufotokonzera kwa zimene mumachita mu kulambira, mukhoza kuyamba kufunsa, "Kodi ndi chifukwa chiyani timachita zimene timachita?" ndipo "Tingachite bwino motani?"

Zisankho zokhudza kulambira zimaonetsera zikhulupiriro zathu pa Mulungu. Zopezeka mu kulambira kwathu zimaonetsa zimene timakhulupirira za Mulungu ndi m'mene timakhalira ndi Iye; zopezeka mukulambira kwathu zimaonetsa zimene timakhulupirira za mpingo komanso m'mene timakhalira ndi wina ndi mzake; zopezeka mu kulambira kwathu zimaonetsera zimene timakhulupirira za otaika ndi m'mene kulambira kukhoza kuwafikira.

Tiyeni tione chitsanzo chimodzi – kuyimba kwa mpingo onse.

- Kusapezeka kwa nyimbo ya mpingo onse mu mpingo wa Katolika zinaonetsera kuti anthu wamba sanazindikire malemba (kuphatikizirapo malemba oyimba). Munthu wamba samaloledwa kuwerenga malemba pawokha, munthu wamba samaloledwa kuyimba nyimbo zamatamando. Kulambira kumachitika ndi wansembe.
- Kutsindika kwa nyimbo ya mpingo onse mu Kukozanso zinaonetsera chikhulupiriro cha Luther chakuti Mkhristu aliyense akhoza kulambira ngati chiwalo cha thupi la Khristu.
- Kukana kwa Calvin kwa nyimbo zina kupatula Masalimo kunaonetsera chikhulupiriro chake chakuti Mawu a Mulungu okha anali ololedwa mu kulambira.
- Kutsindika kwa a Methodist pa nyimbo ya mpingo onse ndi kuphunzitsa chiphunzitso kudzera mu nyimbo zinaonetsera kukhudzika kwa Wesley kwakuti okhulupirira aliyense ayenera kuyimba ndikuti zimene timayimba zimakhudza zimene timakhulupirira.
- Kusavuta kwa malire oyimba zinaonetsa kukhudzika kwa Methodist kuti chipulumutso ndi cha anthu onse. Chifukwa cha kukhudzika kumeneku, anapangitsa aliyense kukhala nawo mu kuyimba.

Pamene tikupitiriza phunziro ili, tikhala tikuona mfundo zambiri za kulambira. Funso lanu loyambirira lokhudza kulambira mwachidziwikire likhoza kukhala, "Kodi ndikuzikonda?" Limenelo sifunso lofunikira. Lofunikira kwambiri ndi, "Kodi kulambira kwanga kumanena

chiyani za zimene ndimakhulupirira? Kodi kumaonetsa kumvetsetsa koyenera kwa ubale wa Mulungu ndi munthu kwa Iye?”

Kulambira kwathu kumasula zimene timakhulupirira, koma mbali inayonso ndiyoona: zikhulupiriro zathu zimasula m’mene timalambirira.

KUBWEREZA KUONANSO PHUNZIRO 5

1. Mu mpingo woyambirira:

    - Kulambira kunali kopanda ndondomeko kokhazikika.
    - Kulambira kunali ndi kutengapo mbali kwa anthu wamba.
    - Kulambira kunatenga mbali zonse za moyo.

2. Mu kulambira kwa zaka za pakatikati:

    - Kukongola kunali kofunikira kuposa uzimu.
    - Anthu samatha kuzindikira mwambo wa mapemphero.
    - Anthu anali owonerera, osati olambira nawo.
    - Uthenga Wabwino unalowedwa m’malo ndi miyambo.

3. Mukukozanso:

    - Kulambira kunaonetsa unsembe wa okhulupirira.
    - Kulambira kunali muchiyankhulo cha anthu.
    - Luther, Calvin ndi Puritans sanagwirizane pa ntchito ya miyambo mu kulambira.

4. Mu Mipingo ya Ufulu motsatira Kukozanso:

    - Ulaliki chinali cholinga chachikulu.
    - Kutengapo mbali kwa anthu kunali kofunikira.
    - Chiphunzitso cha unsembe wa okhulupirira chinali chofunikira.
    - Mwambo onse wa kulambira unali mu chiyankhulo cha anthu.
    - Kudziimira kodutsa malire kwa munthu payekha kunali koopsa.

5. Kulambira kwa Methodist koyambirira kunadziwika ndi:

    - Kutsindika kwa ulaliki
    - Kutsindika kwa Mgonero wa pafupipfupi
    - Kutsindika kwa kuyimba nyimbo
    - Kutsindika kwa magulu ang’onoang’ono
    - Kutsindika kwa kulambira kwa gulu
    - Kutsindika kwa ulaliki chisokole

6. Kulambira mu America Oyambirira:

   - Analimbikitsa kutengapo mbali ndi kukhudzika mu ulaliki chisokole
   - Nthawi zina anatsindika za chidziwitso chamunthu pa chiphunzitso

7. Kulambira kwathu lero kumaonetsa zikhulupiriro zathu pa Mulungu ndi m'mene timakhalira ndi Iye.

NTCHITO YA PHUNZIRO 5

1. Justin Martyr anafotokozera kulambira kwa zaka zana za chiwiri mu ndime zochepa. Amalembera kwa wina wake amene sanaonepo kulambira kwa Chikhristu. Lembani ndime ziwiri kapena zitatu zimene mufotokozere kulambira kwanu kwa Chikhristu kwa wina wake amene sanakhale mu mpingo wa Chikhristu. Mosamalitsa ganizirani zimene zili zofunikira za kulambira kwanu. Kodi mungafotokozere motani kulambira kwanu munjira yakuti ikhoza kupereka uthenga ofunikira wa kulambira kwa Chikhristu?

   Ngati mukuphunzira pa gulu, kambiranani mayankho a wina aliyense wa pagulu mu mkumano wanu wotsatira.

2. Kumayambiriro aphunziro lotsatira, mudzakhala ndi mayeso ochokera muphunziro ili. Werengani mafunso a mayeso mosamala pakukonzekera.

MAYESO A PHUNZIRO 5

1. Tchulani zinthu zitatu za kulambira m'zaka za m'zana loyamba zofotokozeredwa Justin Martyr.

2. Fotokozerani zifooko zitatu za kulambira mu Zaka za Pakatikati.

3. Kodi mfundo ziwiri zoyambirira zokhudza Kukozanso unsembe wa okhulupirira ndi ziti?

4. Sankhani (ma)gulu mu Kukozanso zimene zikugwirizana ndi kufotokozera kwake.

   - Analola mwambo wina ulionse wa kulambira umene unaletsedwa m'malemba: _____
   - Sanalole mwambo wakulambira umene sunafotokozeredwe m'malemba _____
   - Anakana miyambo yambiri. Nthawi zina analambira mu nyumba zawo: _____

5. Tchulani zinthu zitatu zooneka za kulambira kwa mpingo mwa ufulu.

6. Tchulani zinthu zitatu zimene amakhazikikapo wolambira oyambirira a chi Methodist.

7. Tchulani machitidwe atatu a kulambira mu America m'nthawi zoyambirira.

8. Lembani Masalimo 100:1-5 kuchokera pakuloweza.

PHUNZIRO 6

NYIMBO MU KULAMBIRA

ZOLINGA ZA PHUNZIRO

1. Kuzindikira zolinga za Baibulo, ndi za umulungu, ndi zochitika za nyimbo pa kulambira.
2. Kuzindikira kuti nyimbo zimayankhula ku maganizo, ku mtima, ku thupi ndi ku malingaliro.
3. Kudzipereka ku Mfundo za Baibulo zimene zimalondolera chisankho cha nyimbo pa kulambira.
4. Kugwiritsa ntchito mfundo za Baibulo ku mafunso akukhudzana ndi nyimbo pa kulambira.

KUKONZEKERA PHUNZIRO ILI

Lowezani Akolose 3:15-17.

CHIYAMBI

Matthew akufuna kutula pansi udindo wa ubusa pa mpingo wake. Anafika pa mpingo wa Lakeside First ndi chimwemwe chachikulu komanso chikhulupiriro. Amakonda kuwerenga ndi kukonzekera za ulaliki. Amakonda kuyendera anthu ndi kubweretsa chiyembekezo kwa iwo amene ali muzowawa. Ndi okondwa kukhala ndi mwayi ogawana uthenga wabwino ndi anthu osakhulupirira. Anthu a mu mpingo wake amakondwa ndi ulaliki wake. Anthu atsopano akubwera kudzakhala nawo. Matthew akuyenera kukhala osangalala ngati m'busa. Koma china chake ndi cholakwika. Zonse zikubwera chifukwa cha kulimbana pa nyimbo.

Mmawa wa tsiku Lolemba lililonse, Josia amayimbira ku ofesi ya mpingo. "Abusa, nyimbo za dzulo sizinali zosakhala bwino! Sindinadziwe nyimbo yomaliza. Chida choimbira chinali

chokwera kwambiri. Sindingakwanitse kupilira. Mukuyenera kuchitapo kanthu za nyimbo mu mpingo uwu!”

Kenako tsiku Lachiwiri lililonse, Matthew amakumana ndi mtsogoleri wake wa zoyimba, Thomas. Thomas ali ndi chodandaula cha mtundu wina. “Abusa, kodi ndi chifukwa chiyani tikumayimba nyimbo zambiri za kale? Kwaya yatopa nazo nyimbo izi. Tsiku la Mulungu, tinayimba nyimbo ziwiri zakale, ndi imodzi yatsopano. Kodi sitingathe kuzisiya nyimbo zimenezi? Mipingo ikuluikulu yonse inasintha. Chonde ndiloleni ndisinthe nyimbo!”

Pofika usiku wa tsiku Lachiwiri, Matthew akumva ngati asiye. Mbali imodzi ya mpingo wa Lakeside First umakonda nyimbo zakale; amadandaula nthawi zonse nyimbo yatsopano ikayimbidwa. Mbali ina ya mpingo wa Lakeside umadana ndi nyimbo zakale. Matthew sakupeza yankho.

» Kodi mungapereke malangizo otani kwa m’busa Mathew? Kodi nyimbo za mpingo wake zimatumikira motani ku gulu lililonse la mpingo wake?

ZIFUKWA ZIMENE NYIMBO ZILI ZOFUNIKA PA KULAMBIRA

Atafunsidwa zokhudza nyimbo mumpingo, abusa tsiku lina anati,” Sitisoweka nyimbo pa kulambira. Ngati ndimalalikira Mawu a Mulungu mwamphamvu, kuyimba ndikosafunikira.” Abusa awa sanaone phindu lililonse la nyimbo mu kulambira.

» Kodi mungawayankhe motani abusa awa? Kodi ndi chifukwa chiyani nyimbo zili zofunikira pakulambira?

Akhristu ndi anthu oyimba. Asilamu sakumana pamodzi kuti ayimbe. Mabudda sakumana pamodzi kuti ayimbe. Mahindu sakumana pamodzi kuti ayimbe. Akhristu amakumana pamodzi kuti ayimbe. Si Mkhristu aliyense amene amalalikira, kutsogolera pemphero, kapena kuwerenga mawu pagulu. Akhristu onse akhoza ndipo akuyenera kuyimba. Apa pali zifukwa zochepa zakuti nyimbo ndi zofunikira pa kulambira kwa chikhristu.

Zifukwa za Baibulo za Nyimbo pa Kulambira

Nyimbo ndizofunika pakulambira chifukwa nyimbo ndi zofunikira mu Baibulo. Pali maumboni wokwana pafupifupi 600 wokamba zoyimba ndi nyimbo mu malemba. Mabuku 44 Baibulo amakamba za nyimbo.

Nyimbo za mu Baibulo zokhudzana ndi miyambo yosiyansiyana:

- Aisraeli anatamanda Mulungu pa chipambano chawo pa a nkhondo a Farao (Ekisodo 15).
- Aisraeli anatamanda Mulungu atapambana ndi a Jabin (Oweruza 5).

- Woyimba analambira pakuperekedwa kwa kachisi (2 Mbiri 5:11-14).
- Woyimba anatsogolera kulambira pa nthawi yakumanganso kwa Kachisi (Ezra 3:10-12).
- Buku la Masalimo ndi msonkhamsonkha wa nyimbo za kulambira kwa Chiyuda ndi Chikhristu.
- Yesu ndi ophunzira anayimba nyimbo pa Mgonero womaliza (Mateyu 26:30).
- Paulo ndi Sila anayimba zoyamika ali mundende (Machitidwe 16:22-25).
- Yohane anaona kuti kuyimba ndi gawo lina la kulambira kumwamba (Chivumbulutso 4 ndi 5).

Zolinga za Umulungu za Nyimbo mu Kulambira

Wolambira a Chiyuda anayimba pamene anali kulambira. Akhristu oyambirira anayimba odzala ndi chiyamiko kwa Ambuye m'mitima mwawo (Akolose 3:16). Nyimbo zinali mbali imodzi yofunika kwambiri pa kulambira kwa Chikhristu.

Mwatsoka, mu chaka cha A.D 367, bungwe la Laodekiya linaletsa kuimba kwa mpingo onse. Mpingo wa Katolika sunalole anthu wamba kuwerenga Baibulo; mpingo unakhulupirira kuti, ansembe okhawo amene anaphunzitsidwa ndiwo anali ndi kuthekera komasulira Mawu a Mulungu. Chifukwa chomwechi chinapangitsa bungweli kuthetsa kuimba kwa mpingo onse." Ngati munthu okhulupirira alibe kuthekera, kapena mwayi wokwanitsa kutanthauzira malemba payekha, asaloledwenso kuimba nyimbo za mu mpingo."[42] Nthawi ya Zaka za Pakatikati, okhawo amene anaphunzitsidwa zoyimba kwaya ndi amene amayimba mumpingo pa kulambira; okhulupirira wamba anali owonerera.

Chinthu china chofunika kutsimikiza cha za Mulungu cha Kukonzanso, chinali unsembe wa wokhulupirira. Aliyense wokhulupirira ali ndi mwayi ndi udindo wofika yekha kwa Mulungu kudzera mu pemphero; Mkhristu aliyense safunika wansembe kuti atumikire ngati mkhalapakati. Wokhulupirira aliyense ali ndi mwayi ndi udindo womvera Mulungu akuyankhula kudzera mu Mawu ake, ndipo wokhulupirira aliyense ali ndi mwayi komanso udindo woyimba pa kulambira.

Martin Luther anaona kulumikizana kwa pakati pa kuwerenga malemba ndi kuyimba. Iye anati, "Mulekeni Mulungu ayankhunkhule mwachindunji kwa anthu ake kudzera mu malemba, ndipo anthu ake avomere ndi nyimbo za mayamiko."[43] Nyimbo mu mpingo zimaonetsa mfundo za umulungu za **unsembe wa wokhulupirira.**

Mfundo ya chiwiri ya umulungu yowonekera mu nyimbo ndi **umodzi wa mpingo**. Umboni wochuluka wa zoyimba mu Baibulo ndi kuyimba kwa mu mpingo, kuyimba kwa anthu

42 David Jeremiah. *Kulambira* (CA: Turning Point Outreach, 1995), 52.

43 Quoted in David Jeremiah, *kulambira* (CA: Turning Point Outreach, 1995), 52.

onse. Paulo analamula akhristu akale kuti aphunzitsane ndi kuchenjezana ndi nyimbo (Akolose 3:16). Pamene mpingo uyimba pamodzi, timaonetsa umodzi wa mpingo.

ZOOPSA ZA KULAMBIRA: KUSOWEKA KWA NYIMBO ZAMPINGO ONSE

Nyimbo yabwino ya Isaac Watt ikuti,

"Alekeni akane kuyimba iwo amene sanadziwe Mulungu wathu. Koma ana a Mfumu yakumwamba amayankhula za chimwemwe chawo mokweza!"[44]

Martin Luther anati, "Ngati palibe wina amene sangathe kuyimba kapena kunena zimene Khristu watichitira, awonetsa kuti samakhulupirira kwenikweni."[45] Mwayi wa nyimbo umene unatayika mu Zaka za Pakatikati unabwerera ndi Okozanso. Anakhulupirira kuti kulambira mu nyimbo ndi kwa anthu. Zachisoni, m'mipingo yambiri mwayi uwu udatayikanso.

Maonetsedwe a nyimbo za unsembe wa wokhulupirira waopsezedwa ndi nyimbo zimene sizikufikira oyimba wamba. Izi zimachitika ngati kwaya yophunzitsidwa ikuyimba nyimbo zovuta kwambiri kwa anthu ambiri. Zimachitika pamene oyimba akuyimba nyimbo zatsopano zimene ochepa okha akukwanitsa kuzidziwa. Tisalole kuti magulu ochepa alowe m'malo mwa nyimbo ya mpingo onse.

Maonetsedwe a umodzi wa mayimbidwe mu mpingo uli pa chiopsezo m'mipingo chimene chikugawa mpingo muzigawo zosiyana kuchokera pa kulambira kosiyana kapena kusiyana kwa mibadwo. Ndi zovuta kuona mpingo monga thupi limodzi pamene anthu akuluakulu a thupi ili sakutha kuona achichepere.

Taganizani za njira za Paulo ku mpingo wa kwa Aefeso kutanthauziranso ku mipingo ina yamakono:

- Iwo amene amayimba masalimo adzakumana la Sabata nthawi ya 8:30 mmawa.
- Iwo amene amayimba nyimbo adzakumana pa tsiku la Sabata nthawi ya 11:00 mmawa.
- Iwo amene amayimba nyimbo za uzimu akumana tsiku Loweluka nthawi ya 7:00 madzulo.

---

44 Isaac Watts, "We're Marching to Zion." Inapezedwa January 12, 2023. https://library.timelesstruths.org/music/Were_Marching_to_Zion/

45 Zotengedwa kuchokera mwa Ronald Allen and Gordon Borror, *Worship: Rediscovering the Missing Jewel* (Colorado Springs: Multnomah Publishers, 1982), 165.

Ayi! Paulo amayankhula kwa *onse* mamembala a mpingo, amene anawadandaulira kuti akhale odzala ndi mzimu, kuyankhulana wina ndi mzake za masalimo ndi nyimbo ndi nyimbo za mzimu, kuyimba ndi kupanga mingoli kwa Ambuye (Aefeso 5:18-19).

Muzochitika, izi zikutanthauza kuti, gawo lililonse la thupi la Khristu ligonjere zina mwa zofunika zake chifukwa cha umodzi wa thupi. Wachinyamata akuyimba mayimbidwe osasangalatsa. Chifukwa chiyani? Chifukwa iyeyu ndi gawo lina la thupi, ndipo thupili likuyimba nyimbo yakale. Woyera mtima wachikulire wayamba nawo kuyimba nyimbo yatsopano imene iye sikumusangalatsa. Chifukwa chiyani? Chifukwa iye ndi gawo lina la thupi, ndipo thupili likuyimba nyimbo yatsopano.

Munthu wina wophunzitsidwa kuyimba pa mpingo waung'ono ku dera lina, amayimba nyimbo zosavuta. Chifukwa chiyani? Chifukwa iye ndi gawo lina la thupi, ndipo ndi thupi limene mulinso ena amene sayamika nyimbo zapamwamba. Wina osaphunzira bwino wa mutchalitchi akhoza kunena "Amen" komalizira kwa nyimbo yomwe yayimbidwa, munjira yoonetsa kusakhutitsidwa. Chifukwa chiyani? Chifukwa iye ndi gawo lina la thupi, ndipo thupili mulinso ena amene amayimba nyimbo koposa mmene iye angayamikire.

Mfundo iyi imadutsa pa nyimbo. Abusa amapangitsa uthenga wawo kukhala osavuta kumvetsa ndi kwa ana ndi okhulupirira atsopano. Okhulupirira atsopano amaphunzira kumvetsetsa ulaliki umene umatambasula chidziwitso chawo chochepa cha Baibulo.

Achinyamata akhala mu mwambo wa mapemphero umene ukuoneka wa utali. Chifukwa chiyani? Chifukwa akudziwa kuti ndi mbali imodzi ya thupi ndipo akudziwa kuti zochitika zina za mwambo wa mapemphero zikhoza kukhala zoposa chidziwitso chawo. Woyera mtima achikulire akulandira mwana amene amalira mokweza mu mwambo wa mapemphero. Chifukwa chiyani? Chifuk iwo ndi mbali imodzi ya thupi ndipo akukondwera kuti thupi mumakhala achichepere, moyo wa phokoso.

Kodi iyi ndi mbali imodzi ya kulambira? Kwambiri! Chikhulupiriro cha Baibulo cha umulungu chimaphatikiza kuzindikira umodzi wa mpingo. Izi zikutanthauza kuti kusiya zinthu zako zofunika chifukwa cha thupi. Zikutanthauza kuyimba nyimbo imene siikukusangalatsa. Kwa atsogoleri, zikutanthauza kusankha nyimbo zimene zitumikire zigawo zonse za thupi, osati nyimbo zozangalatsa zokha. Nyimbo zanu mpingo onse zikuyenera kutumikira ku mpingo onse, osati gulu lochepa lokha.

» Taganizani za nyimbo zimene mwagwiritsa ntchito pa kulambira pa masabata anayi apitawo. Kodi munayimba nyimbo zimene ziyankhula ku mbali zonse za mpingo wanu? Ngati mtsogoleri, kodi mwakhala mukufuna nokha kusankha nyimbo zimene sizikusangalatsani, koma zimene zimayankhula ku mpingo? Kodi nyimbo zanu zimaonetsa unsembe wa wokhulupirira ndi mgwirizano mu tchalitchi polimbikitsa anthu a mu tchalitchi kutengapo mbali?

ZIFUKWA ZIMENE NYIMBO NDI ZOFUNIKA POLAMBIRA (KUPITIRIZA)

Zifukwa Zodziwika bwino za Nyimbo Pa Kulambira

Kuphatikiza ndi zifukwa za Baibulo komanso za Umulungu, pali zifukwa zooneka zina zimene zili zaphindu ku nyimbo pa kulambira. Mphamvu za nyimbo zimachokera mukuthekera kwake koyankhula mbali zonse za kukhala kwathu.

Nyimbo zimayankhula ku maganizo.

Aphunzitsi amadziwa kuti kuyika lamulo la malemba m'mayimbidwe osavuta kumapangitsa ana kuloweza mawu mosavuta. Kuyimba kwa malemba kumapangitsa kuti zikhale zosavuta. Anthu ena amene amati, "Sindingathe kuloweza Baibulo" amadziwa mavesi ambiri a mmalemba; amayimba nyimbo za matamando. Nyimbo zina zabwino za matamando ndi zochokera ku mavesi a mmalemba zoikidwa mu m'mingoli yachikumbutso.

Mfundo ziwiri zogwirizana ndi nyimbo komanso maganizo ndi zofunika.

1. **Nyimbo ziyenera kuyankhula ku maganizo, osati maimvaimva okha.**

Nyimbo zimakhudza; ili ndi gawo lina la mphamvu zake. Palibe cholakwika ndi mphamvu ya kukhudzika, koma nyimbo ziyenera ziyankhule ku maganizo athu.

Wolambira ena amaganiza kuti akhoza kutseka maganizo awo akamayimba. Gitala ndiyokwera kwambiri, kugunda kwa nyimbo ndi kwamphamvu, nyimbo ndi zokhudza, ndipo amaganiza kuti akupembedza. Tisamayiwale kuti Paulo anati, "Ndidzapemphera ndi mzimu wanga komanso ndidzapemphera ndi nzeru zanga" (1 Akorinto 14:15).

Pamene nyimbo zathu zikuyankhula kumaimvaimva popanda kuyankhula ku maganizo, tili pachiopsezo cha kupembedza konama. Palibe cholakwika ndi nyimbo zimene zikuyankhula kumaimvaimva; choopsa ndi nyimbo zimene zimayankhula kumaimvaimva osayankhula ku maganizo. Abusa anzeru adzaonetsetsa kuti nyimbo za matamando zisadutse maganizo.

2. Uthenga umene timayimba uzikhala owona.

Nyimbo zimayankhula kumaganizo, chomwecho nyimbo ndi chida champhamvu chophunzitsira chiphunzitso. Chifukwa chimodzi chimene uthenga wachilimbikitso cha chipulumutso ndi chisomo wofalikira kwa onse inali mphamvu za nyimbo za Charles Wesley. John Wesley analalikira kuti chisomo cha chipulumutso cha Mulungu ndi chaulere kwa munthu aliyense; nyimbo ya Charles "Kodi chingagulidwe" inabweretsa uthenga kwa mlimi amene samatha kuwerenga malemba a mawu a Mulungu:

"Chonse ndi chifundo, chomiza ndi chaulere,
Cha Mulungu, O chinandipeza."[46]

Abusa, ngati mulola nyimbo zosakhudzana ndi Baibulo, mukuchepetsa mphamvu za mphamvu ya utumiki wanu. Anthu adzakumbuka nyimbo nthawi atayiwala za ulaliki wanu. Khalani ndi nthawi kukonzekera za nyimbo pa utumiki. Onetsetsani kuti nyimbo zikuthandizira choonadi cha ulaliki.

Wa Methodist ayimbe "ngati njira yokwezera mzimu wodzipereka, wakutsimikiza za chikhulupiriro chake, kulimbikitsa za chiyembekezo, kukulitsa chikondi chake cha pa Mulungu ndi munthu."

John Wesley

FUFUZANI

Kodi nyimbo zanu za matamando ziima pa zoonadi cha chiphunzitso cha za mu Baibulo? Matchalitchi ambiri amayimba nyimbo zimene zimaphunzitsa zolakwika ***kapena*** osaphunzitsa kanthu (mawu opanda tanthauzo). Kodi nyimbo zanu zimaphunzitsa zoona zenizeni za chipambano pa tchimo? Kodi nyimbo zanu zimaphunzitsa kuti chipulumutso ndichopezeka kwa aliyense? Kodi nyimbo zanu zimaphunzitsa za lonjezo la mtima wangwiro?

46 Charles Wesley, "Kodi chingagulidwe?" inafufuzidwa pa January 12, 2023. https://library.timelesstruths.org/music/And_Can_It_Be/

Nyimbo zimayankhula ku mtima.

Jonathan Edwards anati tinalamulidwa kuyimba nyimbo za matamando kwa Mulungu chifukwa kuyimba "kumasuntha maimvaimva athu."[47] Pamene chidwi pa maimvaimva okha ndi koopsa, maimvaimva ndi abwino komanso oyenera ku nyimbo. Kuyimba kumabweretsa kuvomereza ku choonadi. Nyimbo zimayankhula ku maganizo ndi mtima.

Akhristu ena akumayiko a azungu amaopa nyimbo zimene zimayankhula mozama ku maimvaimva, koma anthu a mu Baibulo amene analowa mu kupezeka kwa Mulungu anamva kukhudzika kwa maimvaimva. Nyimbo zabwino za matamando zimayankhula ku maganizo ndipo zimafuna kuvomera kochokera mu mtima.

Khalani ndi njira Yanu, Mbuye! Khalani ndi njira yanu, Mbuye!
Inu ndinu owumba, Ine ndine dothi.
Mundiumbe ndi kundipanga chimene Mufuna,
Pamene ndikudikira, woyembekezera ndi kudekha.[48]

Nyimbo zimayankhula ku thupi.

Taonani mwana ku malo ovina; ngati nyimbo zikumveka kugunda, amayamba kusuntha. Nyimbo zimayankhula ku thupi.

Nyimbo zimene zimayankhula ku thupi kokha ndi zokometsa thupi. Komabe, pamene Baibulo likukamba zakulambira, nthawi zambiri limakamba za maimidwe a thupi a wolambira: kukweza manja, mawondo ogwada, matupi ogona, ndi mayendedwe a mphamvu. Kuyima kwathu kwathupi ndi machitidwe athu nthawi zina kumanena kwambiri mwa mphamvu kuposa mawu athu.

Mu Masalimo 149:3, Israeli akuitanidwa kuti "alambire dzina lake ndi mavinidwe, kupanga mingoli ya Iye ndi lingaka ndi pangwe." Ngakhale miyambo ya makono imavina mosangalatsa thupi; Baibulo limagwiritsa mawu a *kuvina* kunena za kugwedezeka kulikonse kwa thupi pa kulambira. Wolemba masalimo akuzindikira kuti ngakhale thupi limakhudzidwa pa kutamanda.

Uku sikuvina kosangalatsa thupi kumalo omwera mowa, komanso sikukhala chete mwadongosolo. Kuvina kwa mu Baibulo kumakhudza mulingo wina wake wakusuntha mu nthawi ya nyimbo za kulambira. Pamene tikweza manja athu kumwamba polambira kapena kuyenda motsatana ndi nyimbo, zimagwirizana ndi zochitika za Baibulo *kuvina*.

---

47 Mawu ofotokoza mwachidule ochokera kwa Bob Kauflin, *Worship Matters* (Wheaton: Crossway Books, 2008), 98.

48 Adelaide Pollard, "Khala Have Thine Own Way, Lord." Inafufuzidwa January 12, 2023. https://library.timelesstruths.org/music/Have_Thine_Own_Way_Lord/

Pamene tanthauzo losonyeza zochitika zimasiyanasiyana malinga ndi kusiyana kwa makhalidwe komanso mibadwo-mibadwo, tisalole kuti kulambira kopatulika kwa Mulungu kupangidwe mofanana ndi makhalidwe oyipa amene azungulira chikhalidwe chathu.

» Onani Eksodo 32 kulambira kumene kunaphatikiza chotchedwa "chikondwelero cha Ambuye" (32:5) ndi mafano onyasa a kulambira kwa Aigupto amalambira (32:4) ndi chikhalidwe chochititsa manyazi chopembedza mafano (32:25). Kulambira kwathu kuyenera kuzikhudza chikhalidwe chotizungulira kudzera mu chisokole. Chikhalidwe chotizungulira chimapanga machitidwe athu a kulambira.

Abusa anzeru ndi atsogoleri adzapeza nyimbo zimene zikupewa malambiridwe onyasa, ndi kupeza nyimbo zimene zimayankhula kwa munthu yense, kulola mpingo onse kuti ulambire moonadi munyimbo.

FUFUZANI

Kodi nyimbo zanu za matamando zimalankhula ku thupi mukhalidwe loyenerera lotamanda? Kodi otamandira anu amaonetsera muthupi za kulambira ndi kutamandira kwao posanyasitsa matamando ndi kupanga za chikhalidwe chosangalatsa matupi?

Nyimbo zimayankhula ku malingaliro.

Nthawi zambiri nyimbo zimafuna kuyankha kwa Malingaliro. Paulo analamulira Akolose kuti aziphunzitsana ndi kulangizana wina ndi mzake pakuyimba Masalimo, nyimbo zotamanda ndi nyimbo zauzimu (Akolose 3:16). Kulangiza ndi kukonza cholakwikwa. Chidzudzulo chimafuna yankho; chidzudzulo chimafuna munthu kuti asinthe khalidwe lake. Paulo anayembekezera nyimbo kukhala chopangitsa kusintha.

Kunja kwa mpingo, timaona mmene nyimbo zimayankhulira ku malingalro. Pamene anthu akuda aku America (amadziwitsa anthu za ufulu wao mu zaka za m'ma 1960) anayimba "Tidzagonjetsa," Nyimboyi imayankhula ku mitima yawo ndi ku malingaliro. Nyimbo iyi inakhala ngati yoyitanira, "Kodi mungakhale nafe mu nkhondo yomenyera ufulu?"

Nyimbo imayitanira malingaliro ku yankho. Ganizirani za kudzipereka kumene kumakhalapo tikamayimba:

"Tengani moyo wanga ndipo zitero
Wopatulidwa, Mbuye kwa Inu.
Tengani nthawi yanga ndi masiku anga;
Ziyende mmatamando osatha.

Tengani manja anga lolani ayende
Pakugunda kwa chikondi chanu.
Tengani mapazi anga ndipo akhale
A changu ndi abwino kwa Inu.

Tengani chifuniro changa chikhale Chanu;
Sichizakhalanso changa.
Tengani mtima wanga—ndi Wanu,
Ukhale mpando wanu wa Chimfumu."[49]

Nyimbo ndi yofunika pa kulambira chifukwa imakamba za munthu yense. Chifukwa cha ichi, nyimbo ndi yofunika komanso yoopsa. Ndiyofunika chifukwa imatha kupereka choonadi munjira yamphamvu. Ikhoza kukhala yoopsa chifukwa zikhoza kupereka chiphunzitso chonama kukhala ndi chikoka. Warren Wiersbe anachenjeza, "Ndili otsimikizika ku mipingo imaphunzira za Mulungu zambiri (zabwino ndi zoipa) kuchokera mu nyimbo zimene amayimba kusiyana ndi ulaliki umene amamva… [Nyimbo] zikhoza kukhala chida chodabwitsa mmanja mwa Mzimu kapena chida zoopsa mmanja mwa Mdani. **Mipingo yosadziwa ikhoza kuyimba mwa njira asanazindikire zimene zikuchitika**."[50]

Nyimbo ndi zamphamvu; zigwiritseni ntchito mwanzeru.

---

49 Frances Havergal, "Take My Life and Let It Be." Zatengedwa pa January 12, 2023. https://library.timelesstruths.org/music/Take_My_Life_and_Let_It_Be/

50 Warren Wiersbe, *Real Worship* (Grand Rapids: Baker Books, 2000), 136. Emphasis added.

FUFUZANI

Ganizani za nyimbo zimene mwayimba masabata anayi apitawo. Kodi munayimba nyimbo zimene zinayankhula kwa munthu yense?

- Tchulani nyimbo imene imaphunzitsa chiphunzitso ku mpingo kwanu.
- Tchulani nyimbo imene inayankhula mozana kumaimvaimva a mpingo wanu.
- Tchulani nyimbo imene inasuntha mpingo wanu kupita kukudzipereka kozama kwa Mulungu.

MFUNDO ZOSANKHIRA NYIMBO ZA KULAMBIRA

Tinayamba phunziroli ndi nkhani zotsutsana pa za nyimbo za matamando. Ngati inu muli m'busa amene akukumana ndi kutsutsana kotere, zindikirani kuti ili si vuto latsopano! Mu m'badwo uli wonse, mpingo walimbana ndi kuti uganizire za mtundu wa nyimbo umene uli oyenera pa kutamanda. Kwa mipingo yambiri, nyimbo zakhala chiyambi cha mikangano mmalo mokhala njira ya kulambira koona.

Nyimbo ndiyofunikira pa mwambo wa chipembedzo. M'mipingo yambiri, gawo latheka la mapemphero limakhala lokhudzana ndi nyimbo: nyimbo zakalambula bwalo, nyimbo za mpingo onse, nyimbo zapadera, nyimbo zomalizira, ndi nyimbo zapansipansi nthawi ya chipembedzo. Chifukwa nyimbo ndi zofunikira pa chipembedzo, zotsutsana pokhudza nyimbo zimakhala zozama.

Anthu ali ndi zokonda zazikulu pa za mitundu ya nyimbo. Anthu ena sakonda kutengera nyimbo zimene siziwasangalatsa.

Kutsutsana kumabwera chifukwa cha kusiyana maganizo a za kusiyanitsa kwa maimbidwe. Apa pali ziyembekezo zitatu:

1. Anthu ena amakhulupirira kuti maimbidwe a nyimbo zina ndi oyipa. Amasankha kugwiritsa ntchito maimbidwe ena amene amakhulupirira kuti ndi oyera.

2. Anthu ena amakhulupirira kuti maimbidwe a nyimbo ena sangakhale oyipa kapena abwino, ndipo maimbidwe ali onse ndi ovomerezeka. Anthu awa nthawi zambiri amafuna kugwiritsa ntchito maimbidwe a nyimbo achikhalidwe pa kulambira.

3. Ena amakhulupirira kuti maimbidwe ena a nyimbo alibe mbali koma amakhala ndi kukhudza ndi magulu a chikhalidwe amene amakhudzana ndi kufunikira kwawo pa chipembedzo. Anthu awa amasanthula maimbidwe alionse kuona ngati angathandize mpingo kupembedza mu njira imene ili yolemekeza Mulungu.

Mugawo ili, tiona za mfundo za mu Baibulo zimene zimafotokoza za nyimbo mu kulambira kwathu.

Uthenga wa Nyimbo za Matamando Uyenera Kupereka Choonadi Momveka Bwino

Chidwi choyambirira cha malemba chili pa zimene zili mu nyimbo, osati mayimbidwe a nyimbo.

Kusatengera mayimbidwe a nyimbo, nyimbo zimene zili ndi uthenga wabodza (kapena zopanda uthenga) sizoyenera pa kulambira. Warren Wiersbe akuchenjeza kuti mauthenga ambiri "ndi opanda ntchito komanso opanda tanthauzo, osakhala a umulungu."[51] Yeso limodzi la uthenga wathu wa nyimbo ndi, "Kodi munthu wokhulupirira kuti kuli Mulungu m'modzi, Mhindu, kapena Msilamu angayimbe uthenga uwu osasintha mawu?" ngati mungalowetse mmalo dzina la Buddha osasintha uthenga wa nyimbo, ndiwosayenera pa kulambira. Ngati nyimbo siinena choonadi momveka bwino, ndiyosayenera pa kulambira. Ngati nyimbo siyiyankhula choonadi momveka bwino, tifunse kufunikra kwake pa kulambira. Nyimbo zathu zionetsere chikhulupiriro chathu. Ngati sizitero, nyimbo zathu sizidzalozera wolambira kwa Mulungu.

Mvetserani nyimbo yochokera ku malemba:

Tamanadani Yehova
Tamandani Yehova inu a kumwamba
Mutamandeni Iye, inu a mlengalenga
Mutamandeni, inu angelo onse
Mutamandeni, mutamandeni, inu zolengedwa za mmwamba
Mutamandeni, inu dzuwa ndi mwezi

Lamulo la Zaka Makumi Awiri

"Ngati wina anakula akuyimba nyimbo zathu kwa zaka makumi awiri, Kodi amamudziwa motani Mulungu? Kodi angathe kuzindikira kuti Mulungu ndi woyera, wanzeru, wamphamvu zonse, ndi wa ulamuliro? Kodi angathe kuzindikira za ulemelero ndi kufunikira kwa uthenga wabwino?"

Bob Kauflin
Kulambira Kumafunikira

51 Warren Wiersbe, *Real Worship* (Grand Rapids: Baker Books, 2000), 137.

Mutamandeni, inu nonse nyenyezi ndi zowala
Mutamandeni, inu thambo la kumwambamwamba
Ndi madzi a pamwamba pa thambo
Zonse zitamande dzina la Yehova loleni atamande dzina la Ambuye
Pakuti Iye analamulira ndipo zinalengedwa
Iye anaziika pa malo ake ku nthawi za nthawi... (Masalimo 148).

Fanizirani izi ndi nyimbo yatsopano yotchuka:

"Ndi zabwino kuvina ngati mukuvina mu dzina la Yesu
Ndi zabwino kuvina ngati ukuvinira Ambuye..."[52]

Kodi ndi nyimbo iti imene ikulalikira Mawu a Mulungu? Paulo anachenjeza motsutsana ndi kulambira kumene kunali kosayenera. Iye anati, "Ndidzapemphera ndi Mzimu wanga, komanso ndidzapemphera ndi mzimu wanga" (1 Akorinto 14:15). Tikamawerenga nyimbo za malemba, timapeza kuti zimaphunzitsa momveka bwino. Uthenga wa nyimbo zathu za kulambira uzipereka choonadi cha Baibulo.

Fomu yosanthula nyimbo[53]

	KUFOOKA	PAKATIKATI	MPHAMVU
Kodi uthenga ndi owona monga mwa chiphunzitso?			
Kodi uthenga ndi okhulupirika ku machitidwe a Mkhristu?			
Kodi mpingo umvetsa za uthenga?			
Kodi maimbidwe a nyimbo akulingana ndi mawu?			
Kodi maimbidwe ake anyimbo ndi osavuta kuyimba kumpingo?			

52 James Roberson, "Everybody Dance!" Yapezeka pa January 10, 2023. https://genius.com/James-roberson-everybody-dance-lyrics

53 Zotengedwa kuchokera kwa Constance M. Cherry, *The Worship Architect*. (Grand Rapids: Baker Academic, 2010), 202-203.

FUFUZANI

Kodi nyimbo zanu za kulambira ndi zoona mwa Baibulo? Kodi wokhulupirira watsopano adzazindikira Mulungu wa Baibulo mu nyimbo ku mpingo wanu?

Maimbidwe a Nyimbo za Kulambira Akhoza Kukhala Osiyana

Mulungu ndi Mulungu opanda malire. Anauzilira ma uthenga anayi mu chipangano chatsopano, osati umodzi. Anayankhula kudzera mwa anthu apaderadera olemba. Analenga nsomba zamitundumitundu zambiri osati imodzi. Analenga diso lamunthu lothekera kusiyanitsa mitundu 8 miliyoni ya zinthu. Chilengedwe chimaonetsa ulemelero wa Mulungu mu chikhalidwe chake ndi kukongola. Analenga anthu amaonekedwe osiyanasiyana, osati mmodzi ayi. Mulungu amaonetsa zosiyanasiyana zopanda malire.

Nyimbo zathu zionetsere luso la chilengedwe chosiyanasiyana cha Mulungu amene timamulambira. Mu Akolose 3:16 Paulo akuonetsa mitundu itatu ya nyimbo zimene zikuyenera kugwiritsidwa ntchito pa kulambira: masalimo, nyimbo, ndi nyimbo za uzimu (Onaninso Aifeso 5:19). Paulo sanapereke tanthauzo la mayimbidwe atatu awa. Olemba ambiri anatanthauzira izi motero:

- *Masalimo* mwina zikutanthauzira za buku la Masalimo.
- *Nyimbo* mwina ndi nyimbo zolembedwa ndi anthu. Olemba ambiri amachepetsa mawu awa a nyimbo zoyimbidwa kwa Mulungu kapena za Mulungu. Izi zikhoza kuphatikizika ndi nyimbo za mu Baibulo osati buku la Masalimo zokha.
- *Nyimbo za Uzimu* ndizovuta kuzitanthauzira. Olemba ena amatanthauzira ngati nyimbo zomasuka; ena amaganizira kuti nyimbo za uzimu ndi nyimbo zokhudza moyo wa akhristu komanso nyimbo zochitira umboni wa munthu payekha.

Pakusatengera za tanthauzo, ma vesi awa amaonetsa kuti mpingo unayimba nyimbo zosiyanasiyana kuyambira pachiyambi.

Warren Wiersbe akukamba za mfundo zenizeni. Akulemba, “Kuonetsera kwa kulambira kuyenera kukhale koyenera, koonetsera kusiyana kwa chikhalidwe cha anthu.”[54] Kulambira kwenikweni kumayankhula za Mawu amoyo a Mulungu mu chiyankhulo cha chikhalidwe china chili chonse. Mu m’badwo uliwonse, akhristu alemba nyimbo zimene zimayankhula

54 Warren Wiersbe, *Real Worship* (Grand Rapids: Baker Books, 2000), 139.

za kutamanda kwa Mulungu munjira ya maimbidwe a chikhalidwe chawo. Tisanganize kuti nyimbo za chikhalidwe chathu ndizo nyimbo zopatulika zenizeni. Mmalo mwake, mwina ngati maimbidwe atsutsana ndi mfundo zooneka bwino za mu malemba, tiyenera tilole kuti chikhalidwe chili chonse ndi m'badwo uli wonse utamande Mulungu mu chiyankhulo chawo.

FUFUZANI

Kodi maimbidwe ampingo wanu amawonetsa luso lolenga zosiyanasiyana la Mulungu?

Simayimbidwe Onse Amene Ali Ogwirizana ndi Nyengo Iliyonse

Ngakhale anthu ambiri ayesera kutanthauzira maimbidwe a nyimbo a Baibulo, Baibulo sililamula za mtundu wa maimbidwe enieni. Atamaliza kuphunzira za malingaliro, Francis Schaeffer analemba, "Ndiloleni ndinene pang'ono kuti kulibe maimbidwe a umulungu..."[55]

Mamvekedwe a nyimbo sapereka zinthu zoyenera. Mamvekedwe a nyimbo akhoza kukhala aumulungu kapena opanda umulungu. Kodi zikutanthauza kuti maimbidwe a nyimbo aliwonse ndi woyenera kukhala otamandira? Ayi. Maimbidwe ena ndi okhudzana ndi chikhalidwe cha machimo ndipo kuti sangathe kupereka uthenga wa umulungu polambira.

Oyimba ndi atumwi anapeza zinthu zofanana: anthu anachita mosiyana malinga ndi mmene amvera maimbidwe a nyimbo. Ngati anthu awiri akumvetsera nyimbo imodzi, wina akhoza kuyamba kulira chifukwa cha mmene nyimbo yamufikira. Wina sangamve chili chonse ndi mmene nyimbo yikumvekera.[56]

Kuyesa kwakukulu kwa nyimbo za matamando sikungakhale, "Kodi ndayikonda?" kapena "Kodi ikunditsitsimutsa?" kuyesa kwakukulu ndi ulemelero wa Mulungu. Izi zitanthauza kuti tikuyenera kuona zimene maimbidwe a nyimbo akunenena mkatikati mwa chikhalidwe chathu. Tikhoza kufunsa, **"Kodi mkati mwa chikhalidwe changa, kodi maimbidwe awa akulemekeza Mulungu?"**

Mutha kunena kuti, "Zinthu zonse n'zololedwa," komatu si zonse zili za phindu. "Zinthu zonse n'zololedwa," komatu si zonse zimathandiza (1 Akorinto 10:23). Ngati cholinga chimodzi

55 Francis Schaeffer, *Art and the Bible* (Downers Grove: InterVarsity Press, 1973), 51.

56 Gerardo Marti, Worship across the Racial Divide: Religious Music and the Multiracial Congregation. (England: Oxford University Press, 2012).

cha nyimbo za matamando ndikumangilira okhulupirira, maimbidwe athu asatchinge cholinga chimenechi. Nyimbo zomwezi zikhoza kuthandiza kutamandira mu chikhalidwe china, ndipo chiletso ku chikhalidwe china. Mtsogoleri wosamala wa kulambira adzasankha nyimbo zimene zili zoyenera kwa anthu amene akuwatsogolera.

Kodi tingadziwe bwanji ngati maimbidwe ena a nyimbo ndi oyenera? Ngati mtsogoleri, muli ndi udindo wothandiza anthu anu kuzindikira za izi mu chikhalidwe. Zimene zili zoyenera mu chikhalidwe cha ena sizikhala zoyenera kwa ena. Chifukwa cha maimbidwe a chipembedzo okhazikika, kapena chifukwa maimbidwe olumikizana ndi zochitika zamachimo zozungulira pa chikhalidwe, maimbidwe ena sangakhale oyenera polambira. Mukuyenera kusankha nyimbo zoyenera pa zochitika zanu.

Paulo anatilamula ife kuti tiyese chilichonse ndi kugwiritsitsa chimene chili chabwino (1 Atesalonika 5:21). Izi tikunenanso ndi za nyimbo zimene timayimba. Tisavomereze chinthu tisanachiyese ndi kuchivomereza. Izi tikunenenanso ndi za nyimbo zimene timayimba.

FUFUZANI

Kodi mumayimba nyimbo zimene zili zosagwirizana ndi chikhalidwe chanu? Kodi nyimbo zanu zimayankhula za uthenga wosangalatsa thupi kapena machitidwe a dziko **muchikhalidwe chanu**? Kodi uthenga wa nyimbo umatsutsana ndi uthenga wa mmalemba?

Pakhale Kugwirizana mu Nyimbo zathu za Matamando

Buku la Masalimo likuwonetsa kuti Mulungu amakonda kulambira kwa mitundumitundu. Buku la Masalimo muli kutamanda, kukuwa, kulilira thandizo, ndi kuyamika chifukwa cha mamasulidwe. Masalimo akukamba za zinthu zofunika polambira kwa onse opembedza.

Chizindikiro chimodzi choonetsa kukula mu mpingo ndi kusiyana (1 Akorinto 12:4-6). Thupi la Khristu ndilophatikizilana ndi zikhalidwe zosiyana, ziyankhulo zosiyana, anthu osiyana, ndi mphatso zosiyana. Kupemphera kwathu mophatikiza ndi nyimbo, kukuyenera kuyankhula onse a m'thupi la Khristu. Makamaka kulambira kwathu kukuyenera kuyankhula mopitirira pa kupereka uthenga kwa anthu osakhulupirira. Nyimbo za mu Baibulo zimayankhula kwa magulu atatu.[57]

57 Izi zinatengedwa kuchokera kwa Herbert Bateman, wolemba. *Authentic Worship* (Grand Rapids: Kregel Publications, 2002), 150-155.

Nyimbo zikuyenera kulengeza matamando kwa Mulungu: "Imbani ndi kuyimbira Yehova nyimbo zotamanda" (Aefeso 5:19).

» Werengani Masalimo 91.

Masalimo 91 akuonetsa kuti timayimbira Ambuye. Nyimbo zionetse kutamanda kwa Mulungu. Kuchokera ku nyimbo za matamando mu Eksodo 15 kupita ku nyimbo za kumwamba mu Chivumbulutso, nyimbo za mu Baibulo zimatamanda Mulungu chifukwa cha ukulu wake. Cholinga choyambirira mu nyimbo za Baibulo ndi kutamanda. Salimo lolira, lopempha, kapena matamando, nthawi zambiri limapita kwa Mulungu.

Imbani mu buku la Masalimo ndipo mudzayimba:

- "Ndinalira mokweza kwa Ambuye..."
- "Ndiyankheni ndikakuyitanani, O Mulungu wanga wolungama!"
- "Ndidzapereka mayamiko kwa Ambuye ndi mtima wanga wonse."
- "Ndidzayimba kwa Ambuye."
- "Ndimakukondani Ambuye."

Nyimbo ziyenera zilengeze choonadi ku mpingo: "Kuphunzitsa ndi kulangizana wina ndi mzake" (Akolose 3:16).

Atsogoleri ambiri wopemphera ananena kuti, "Tisamayimbe ku magulu ena, tiziyimba kwa Mulungu yekha basi." Komabe, masalimo ambiri amayimbira ana Aisraeli. Ngakhale zili zoona kuti nyimbo zambiri zimayankhula kwa Mulungu, ndi zowonanso kuti nyimbo zambiri mu Baibulo zimayankhula ku mpingo.

Aefeso 5:19 akulangiza wokhulupirira kuyankhula **kwa wina ndi mzake** mu masalimo, nyimbo ndi nyimbo za uzimu. Akolose 3:16 akunena motsimikiza zolinga za maimbidwe athu: "Mawu a Khristu akhazikike kwathunthu m'mitima mwanu, **Muziphunzitsana ndi kulangizana wina ndi mnzake** ndi nzeru zonse pamene mukuyimba Masalimo, nyimbo zotamanda ndi nyimbo zauzimu, kuyimbira Mulungu ndi mitima yoyamika."

GULU LA NYIMBO ZA KULAMBIRA



Paulo akuonetsa kuti Mawu a Khristu akulalikidwa mu nyimbo zoyimbidwa mu mpingo. Pamene tikuyimba, timayankhula ndi choonadi cha Mulungu kwa anzathu wopembedza

nawo. Kudzera mu nyimbo, mpingo umaphunzitsana wina ndi mzake. Kudzera mu nyimbo, wokhulupirira amapangidwa ndipo thupi la ambuye limamangiliridwa.

Nyimbo zilalikire za uthenga wabwino ku dziko lapansi: "Lengezani za ulemelero wake pakati pa maiko..." (Masalimo 96:3).

Wolemba masalimo anatiyitana ku kuyimba ngati umboni ku maiko:

> Imbirani Yehova nyimbo yatsopano; imbirani Yehova, dziko lonse lapansi! Imbirani YEHOVA, tamandani dzina lake; lalikirani chipulumutso chake tsiku ndi tsiku. Lengezani ulemelero wake pakati pa maiko, ntchito zake zodabwitsa pakati pa mitundu yonse ya anthu! (Masalimo 96:1-3).

» Werengani Mafumu 8:41-43.

Pamene Mulungu atamandidwa, uthenga umatchulidwa kwa amitundu. Pamene amatsekulira Kachisi, Solomoni anapemphera kuti ngakhale anthu a mtundu wachilendo azikapemphera mu kachisi; anapemphera kuti dzina la Ambuye lidziwike kwa anthu onse pa dziko lapansi. Pamene tikupemphera, uthenga ukuchulidwa ku dziko limene likuyang'anira.

Nyimbo zathu za matamando ziyankhule kwa Mulungu komanso za Mulungu; nyimbo zathu zamatamando ziyakhule ku mpingo; nyimbo zathu za matamando zilalikire za uthenga wabwino ku dziko lapansi.

Pamene ife tayiwala ena a magulu awa, kutamanda kwathu kumakanika kukwaniritsa cholinga chonse cha Mulungu ku tchalitchi. Pamene tayiwala kuti Mulungu ndiye yekhayo wofunika kuti atimvere, kutamanda kwathu kumakhala kolephera kuyankhula koyambirira ndi Mulungu. Pamene tikuyiwala kuti tchalitchi ndi malo opemphererako, timakanika kuphunzitsana ndi kulangizana wina ndi mzake polambira. Pamene tiyiwala kuti popemphera tiyenera kutchula za uthenga wabwino ku dziko lonse lapansi, timakanika kukwanitsa kukopa ena ndi kukwanitsa Ntchito ya Utumwi.

FUFUZANI

Kodi mu nyimbo zanu mumayankhula ndi Mulungu, ndi mpingo, kapena ndi osakhulupirira? Sinyimbo zonse zimene zimayankhula kwa zinthu zonsezi; koma pomaliza pa zonse, tiyenera kuyankhula ndi lililonse la magulu awa.

KUCHITA

Taona chifukwa chimene nyimbo zili zofunikira pa kulambira. Tayesa mfundo za Baibulo za nyimbo mu kulambira. Timaliza phunziro ili pakuwona za maganizo ochitika pa za nyimbo pakulambira. Mukhoza kutengerako izi ndi kuti zigwirizane ndi mpingo wanu komanso ndi dongosolo la mpingo wanu.

Poyankhapo pa mfundo zomwe zaikidwa pamwamba, wophunzira anafunsa," ngati maimbidwe a nyimbo za matamando ali osiyana ndipo ngati maimbidwe a nyimbo siosangalatsa kapena oyipa, kodi pali ndondomeko zimene zingatsatidwe kutithandiza ife kusankha nyimbo za mpingo wathu?"

Inde, pali ndondomeko zimene zingatithandize. Mukuyenera kukhala otsimikizika mmene mungachitire izi munyengo zanu, koma mfundo zina zikuyenera kutsogolera maganizo athu pa nyimbo za mpingo.

Nyimbo Zofunika Kwambiri za Mpingo ndi Kuyimba kwa Mpingo onse

Chifukwa chakuti nyimbo za mpingo zimaonetsa umodzi wa mpingo komanso unsembe wa okhulupirira, maimbidwe athu ofunikira kwambiri ndi kuyimba kwa mpingo onse. Pamene makwaya, oyimba okha, amatamando, oyimba ndi zida zili zofunika, nyimbo za mpingo ndi zofunikira kwambiri mu kulambira kwa Chikhristu. Pali njira zina zimene tingatenge kuti tikhazikitse nyimbo za mu mpingo.

Kumbukirani:

1. **Zophatikiza zake zisakhale zosokoneza kapena zokwera kwambiri kuti mpaka zichotse chidwi choyimba**. Mu chipangano Chatsopano, kuyimba ndi chinthu choyambirira mu mpingo. Oyimba ndi zida monga piyano, magitala, ng'oma—si ife anyimbo oyambirira mu mpingo. Lekerani mpingo uyimbe!

2. **Nyimbo zina zimayimbidwa bwino popanda kuyimbira zida**. Nyimbo za mapemphero nthawi zina zikhoza kuonetsedwa ndi maimbidwe ofatsa popanda zida. Izi zimalola mpingo kuika chidwi chake pa uthenga wa mawu popanda chosokoneza.

3. **Nyimbo zisakhale zovuta kapena zatsopano zoti mpingo sungathe kuyimba nawo**. Nyimbo zatsopano ndi zabwino, koma tilole kuti mpingo ukhale ndi nthawi

yophunzira bwino nyimbo zatsopano, musanaonjezere nyimbo zina zatsopano. Kuchuluka kwa nyimbo zatsopano kumakhala kotopetsa kufikira sitingatengeponso uthenga. Njira yina yabwino ndikuwonjezera zatsopano pamene tikusunga zodziwika.

4. **Abusa akuyenera kuyimba limodzi ndi mpingo**. Ngati kuyimba kwa mpingo kuli kotamanda, muyenera mutamande. Pamene abusa akupanga zinthu zina nthawi yoyimba mu mpingo, machitidwe akunena kuti, "Ulaliki wanga wokha ndiwo ofunika pa nthawi ya mapemphero." Abusa apereke chitsanzo cholambira ku mpingo.

Nyimbo Iyenera Kugwirizana ndi Uthenga

Popeza nyimbo za kulambira zikuyenera kulengeza matamando kwa Mulungu, kuyankhula choonadi ku mpingo, ndi kufalitsa uthenga wabwino ku dziko lonse lapansi, mawu wolembeka ndiwo chinthu chofunikira kwambiri. Kusatengera za mtundu wa maimbidwe, ngati nyimbo zikutchinga uthenga, sitikuuzana wina ndi mzake mu masalimo, nyimbo ndi nyimbo za uzimu.

Izi sizikutanthauza kuti nyimbo zoyimbira zida sizofunikira. Zida zoyimbira zikhoza kutithandizira poganizira m'maganizo, kukhudzidwa, ndi chikhumbo cholambira. Zida zoyimbira zikhoza kukhala za phindu polambira, koma ku nyimbo za mpingo chidwi chathu choyambirira ndi uthenga.

Mtsogoleri athandize mpingo kuyika chidwi pa tanthauzo la uthenga.

Atsogoleri akhoza kupangitsa uthenga kuti akhale watanthauzo malinga ndi mmene akuwatsogolera. Zitsanzo ziwiri ziwonetsa mmene mtsogoleri amakhalira ndi mphamvu pa uthenga wa nyimbo.

Amosi sakuganizira mosamala za uthenga wa nyimbo za mpingo onse. Sabata yatha, Amosi anatsogolera nyimbo ziwiri zimene zimakamba za Utatu. Poyamba mpingo umayimba, "Bwerani, Inu Mfumu Yamphamvu." Ndipo Amosi anati, "Tiimba ndime yoyamba, yachiwiri ndi yachinayi."

Kodi cholakwika ndichiyani kusiyako ndime yachitatu pa nyimbo iyi? Taonani pa uthenga; ndi nyimbo yokamba za Utatu. Uthenga uwu wachepetsedwa mphamvu ngati musiyako ndime imene ikukhudza mmodzi wa Atatu.

Ndime yoyamba: Bwerani, Inu Mfumu Yamphamvu… (zokhudza Atate)
Ndime yachiwiri: Bwerani, Inu Mawu osandulika Thupi… (zokhuza Mwana)
Ndime yachitatu: Bwerani, Wotonthoza Woyera… (zokhudza Mzimu)
Ndime yachinayi: Kwa Inu, Wamkulu mwa Atatu… (zokhudza Utatu)

Nyimbo yotsatira inali nyimbo ya matamando. Ndime iliyonse inali yotamanda kwa mmodzi aliyense wa mu Utatu. Amosi anati, "Tiyeni tiyimbe ndime ziwiri." Kachiwiri, Amosi anayiwala kuti nyimbo ya Utatu ikuyenera kukhudza onse atatu. Kusiyako ndime ina ya nyimbo osaganizira za uthenga, zimatchingira kulambira kwa mpingo.

Seth akudziwa kuti kuyimba kwa mpingo onse ndi kofunika pa kulambira. Pa tsiku lasabata, anatsogolera nyimbo ina yosadziwika bwino. Anayamba ndikunenena kuti, "Nyimbo iyi ndi yatsopano kwa ife. Mvetserani Masalimo 150, salimo limene nyimbo iyi ikuchokerapo." Ndi mawu ochepa, Seth anathandiza mpingo kuyika chidwi chake tanthauzo la nyimbo yatsopano.

Nthawi ina munthawi ya mapemphero, Seth anatsogolera kolasi ya makono, "Mulungu Wathu ndi Wamkulu." Asanayimbe nyimboyi, Seth anawerenga 1 Timoteyo 1:17; "Tsopano kwa Mfumu yamuyaya, yosafa, yosaoneka, amene Iye yekha ndiye Mulungu, kukhale ulemu ndi ulemelero mpaka muyaya. Ameni." Nyimbo imene mpingo wakhala ukuyimba nthawi zambiri, inapangidwanso mwatsopano pamene anthu wolambira anamva za malemba zimene zinapangitsa nyimbo kukhala ya mphamvu. Kulumikiza nyimbo ku maziko ake a Baibulo kumalimbikitsa kupembedza kwa mpingo.

Ngati mugwiritsa ntchito makina akanema, munthu amene akuyang'anira za makina akanema ali nawo mbali ya utsogoleri wa wolambira.

Mawu amene akuoneka pa kanema akhoza kuthandiza anthu wolambira kuonetsetsa mwachidwi pa uthenga kapena kukhala osokonekera pa uthenga. Munthu otsogolera za kanema ayenera akhale wosamala pa utsogoleri wawo. Mawu olakwika, zolakwitsa ndi makina a kanema, kapena mawu ena a nyimbo amene agawidwa pa malo osayenera, zonsezi zimasokoneza kulambira.

Taonani zitsanzo zitatu izi. Pa chitsanzo choyamba, mawu ena sanalembedwe bwino. Izi zimasokoneza ena mumpingo; maganizo awo azikhala pa zolakwikazo. Osati pa mapemphero. Muchitsanzo chachiwiri, mawu ali pomwepo, koma zigawo za mawu zimapangitsa kukhala zovuta kuona matanthauzo a mawu. Mu chitsanzo chachitatu, woyimba akhoza kumvetsetsa bwino za uthenga wamatamando kwa Mulungu wathu Wamphamvu.[58]

58 Joachim Neander, tr. by Catherine Winkworth, "Praise to the Lord, the Almighty." Zapezedwa pa January 12, 2023. https://library.timelesstruths.org/music/Praise_to_the_Lord_the_Almighty/

CHITSANZO CHOYAMBA

Mayamiko kwa Yehova, wamphamvu zonse, Mfumu ya chilengedwe!
O moyo wanga tamanda Iye, popeza Iye ndiye
moyo wako ndi chipulumutso chako.

CHITSANZO CHACHIWIRI

Mayamiko kwa Yehova,
Wamphamvu, Mfumu ya
chilengedwe! O moyo wanga, tamanda
Iye, popeza Iye ndiye wangwiro komanso
Nonse amene kumumva, tsopano ku Kachisi Wake
yandikirani yandikirani; khalani ndi
Ine kuyang'anira mwachimwemwe!

CHITSANZO CHACHITATU

Mayamiko kwa Ambuye, Wamphamvu, Mfumu ya chilengedwe!
O moyo wanga, yamika,
Iye, popeza Iye ndiye wangwiro komanso!
Nonse amene mukumva, tsopano ku Kachisi Wake yandikirani;
khalani ndi ine kuyang'anira mwachimwemwe!

Kodi ndi njira iti ikukulolani kuti mukhale ndi chidwi pa uthenga wa matamando? Maonekedwe a mawu pa kanema amakhudza mayimbidwe a mumpingo.

Munyimbo za kulambira, nyimbo zimapereka mawu. Popeza izi ndi zoona, atsogoleri a chipembedzo akuyenera kuthandiza Mpingo kuyimba ndi tanthauzo. Zonse izi palibe zimene **zimayambitsa** kulambira; kulambira kumachokera mumtima. Komabe, kuchotsa zolepheretsa kumalimbikitsa wolambira kuyika chidwi pa chinthu choonadi cholambira, Mulungu.

NJIRA ZODZIWIKA ZOPITITSIRA PATSOGOLO NYIMBO YA MPINGO

1. **Phunzitsani kufunikira kolambira mu nyimbo**. Monga mmene akhristu akufunikira kuphunzitsidwa kufunikira kwa pemphero ndi zina zauzimu, akuyenera kuphunzira zimene Mulungu amafunira kuti iwo aziyimba.

2. **Onetsetsani kuti mpingo ukudziwa chifukwa chimene akuyimbira nyimbo**. Ngati ndi pemphero, akumbutseni. Ngati ndi nyimbo yodzipereka, onetserani. Ngati zikuonekera ku uthenga womwe walalikidwa, ziikeni poyera. Anthu adzayimba mwachimwemwe ngati atadziwa chifukwa chimene akuyimbira.

3. **Sankhani nyimbo za mpingo kusiyana ndi nyimbo zoyimba chabe**. Nyimbo za mpingo onse zimakhala zoyimbika ndi mingoli yokumbukika. Ngati mufuna anthu onse ayimbe, ganizirani, "Kodi ana angathe kuyimba nyimboyi akamabwerera kunyumba?"

4. **Tsitsani pansi zokometsera nyimbo**. Musalore amagitala ndi zida zina zibise mawu a mpingo. Mawu okweza kwambiri mu chipindachi azikhala mawu ampingo.

5. **Onani zofanana pakati pa nyimbo za kale ndi zatsopano**.

6. **Gwiritsani ntchito nyimbo zimene zionetse dera lalikulu la zochitika za Mkhristu**. Ngati nyimbo zonse ndi zachimwemwe, simukuyankhulira Akhristu ena ovutika kwa anthu a mpingo. Monga masalimo, nyimbo zathu ziyenera zikhale ndi mawu Akhristu a chimwemwe, Akhristu a chisoni, Akhristu oyesedwa, ndi Akhristu ovutika.

7. **Abusa ndi atsogoleri a mpingo apange maimbidwe achimwemwe** angakhale atamva kuti sayimba bwino. Kuyimba kwapambali kuli bwino kusiyana ndikusayimba. M'busa amene akuona notsi za uthenga pa pa nthawi yakuyimba akunena kuti," Kulambira munyimbo sikofunikira. "Kulambira munyimbo sikofunikira."

8. **Kumbutsani a mpingo kuti ndiwo chida choyamba mu kulambira kwa gulu lonse**. Ngati anthu sakuyimba mwachimwemwe, cholinga cha kuyimba kwa mpingo kumakhala kuti kwakanika. Mpingo uyenera kuphunzitsidwa kuti ndi koyenera komanso ndi udindo wawo kuyimba kuonetsa m'chitidwe wolambira.

KUMALIZA: UMBONI WA GLORIA

Kodi Mulungu amayankhula kudzera mu nyimbo za kulambira? Mvetserani za m'busa wina wochokera ku Taiwan.

Pamene Gloria atalowa mu mpingo mwathu, anali asanamvepo uthenga. Samafunafuna ulaliki; samafuna kukhala Mkhristu. Gloria samayang'ana Mulungu. Koma Mulungu amafuna Gloria!

Gloria anafika ku mpingo kwathu kuti akaphunzire chingerezi. Anamva kuti kumpingo kwathu timaphunzitsa maphunziro a chingerezi mwa ulere, ndiye anabwera kuti adzaphunzire nawo chingerezi. Patsiku lake loyamba kubwera, Gloria anafika mochedwa. Analowa mu chipindamo. Mpingo umayimba kolasi yosavuta Tchalichi chimaimba nyimbo zosavuta kuchokera pa Masalimo 42:1, "Monga mbawala ipuma wefuwefu kufunafuna mitsinje yamadzi, kotero moyo wanga upuma wefuwefu kufunafuna Inu Mulungu."

Patapita chaka, Gloria anapereka umboni:

"Sindikukumbuka chilichonse cha zochitika kupatulako za nyimbo zimene mumayimba pamene ndimakhala pansi. Pamene ndimavetsera za nyimboyo, ndinayambapo kulira. Pa zaka makumi atatu, ndakhala ndili ndi ludzu la Mulungu monga mbawala ikhala ndi ludzu ndi madzi, koma sindimadziwa kuti ludzu langa ndi la chiyani. Ndinayesa kuphunzira; ndinayesa ndalama; ndinayesa kuzisangalatsa; ndinayesa zonse – koma ndinali wopanda kathu. Ndinaganiza zophunzira chingerezi, ndipo ndinabwera kumpingo uno.

"Mmalo mwa chingerezi ndinapeza madzi amene ndimawafuna. Pamene ndinakhala pa mapemphero, ndinalira poganizira kuti Mulungu ndiye pomaliza pa zofuna za mtima wanga. Iye ndiye wopereka chimwemwe chenicheni. Tsiku limenelo, ndinaganiza zopereka mtima wanga kwa Mulungu. Lero, Iye ndiye chipatso cha maso anga."

KUBWEREZA KUONANSO PHUNZIRO 6

1. Kuyimba ndikofunikira polambira kwathu

- Chifukwa nyimbo zinali zofunika polambira mu Baibulo.
- Chifukwa nyimbo imaonetsa mfundo za chiphunzitso cha umulungu cha unsembe wa okhulupirira.
- Chifukwa chimaonetsa mfundo za umulungu a Mawu a Mulungu a umodzi wa mpingo.

2. Nyimbo

- Zimayankhula ku maganizo, ndi cholinga chakuti uthenga oyimbidwa ukhale wowona.
- Zimayankhula ku mtima, ndi kukhudza maimvaimva.
- Zimayankhula ku thupi koma zisatengedwe ku zinthu zamachimo.
- Zimayankhula ku malingaliro ndikuitana kuchitapo kanthu.
- Zimayankhula kwa munthu yense. Izi zimapangitsa kukhala zaphindu pamene zikuphunzitsa choonadi komanso zoopsa pamene zikuphunzitsa zabodza.

3. Mfundo za malemba za nyimbo za kulambira zimakhala ndi:

   - Uthenga wa nyimbo za matamando uyenera kupereka choonadi momveka bwino.
   - Maimbidwe a nyimbo za kulambira akhoza kukhala osiyana. *Paulo akuonanso za salimo. Nyimbo, ndi nyimbo za uzimu. Kuyambira pa chiyambi, mpingo wayimba nyimbo zosiyansiyana.*
   - Simayimbidwe onse amene ali ogwirizana ndi nyengo iliyonse. *Tifunse kuti, "Mu chikhalidwe changa, kodi maimbidwe anyimbo izi akupereka ulemelero kwa Mulungu?"*

4. Nyimbo Ziyankhule kumagulu atatu:

   - Nyimbo zikuyenera kulengeza matamando kwa Mulungu.
   - Nyimbo ziyenera zilengeze choonadi ku mpingo.
   - Nyimbo zilalikire za uthenga wabwino ku dziko lapansi.

5. Mfundo za nyimbo za mpingo zimakhala ndi:

   - Nyimbo zofunikira kwambiri ndi nyimbo za mpingo onse.
   - Nyimbo ziyenera zitumikire uthenga.

NTCHITO YA PHUNZIRO 6

1. Poyamikira nyimbo zosiyansiyana zopezeka pa kulambira, ikani mndandanda wa nyimbo zinayi kapena kupitiririrapo zimene zikukamba za mitu ya zinthu zotsatirazi. Mndandanda wanu ugwiritsidwa ntchito pamene mukulingalira za mwambo wolambira mu phunziro lina nthawi ina. Funani za nyimbo zimene zidzayankhula ku maganizo anu, mtima ndi malingaliro.

   - Nyimbo zinayi za chilengedwe cha Mulungu
   - Nyimbo zinayi za Kufa ndi kuuka kwa Yesu
   - Nyimbo zinayi za Mzimu Woyera ndi mpingo
   - Nyimbo zinayi zimene zimayitana anthu a Mulungu ku moyo wogonjera, woyera
   - Nyimbo zinayi za chisokole ndi utumwi

   Ngati mukuwerenga pa gulu, gawanani za mndandanda wanu ndi kukambirana, “Kodi ndi nyimbo zingati zimene tayimba mu chaka chapitachi? Kodi tikutchula za uthenga wonse mu mayimbidwe athu?”

2. Poyambirira pa phunziro lotsatira, mudzalemba mayeso molingana ndi phunziro ili. Werengani mafunso mosamala pokonzekera.

MAYESO A PHUNZIRO 6

1. Lembani mndandanda wa nyimbo zitatu zochokera mu Baibulo.
2. Kodi ndi zikhulupiriro zotani zimene zinapangitsa Bungwe la Laodekiya kuletsa kuyimba kwa mpingo onse?
3. Tchulani zinthu ziwiri za maphunziro a za Baibulo zimene ziyenera kuonetsedwa mu nyimbo za kulambira.
4. Tchulani mndandanda wazifukwa zochitika zinayi za nyimbo zolambira.
5. Tchulani mfundo zinayi zimene ziyenera kutsogolera chisankho chathu cha nyimbo.
6. Kodi ndi mitundu itatu iti ya nyimbo imene yatchulidwa ndi Paulo pa Akolose 3:16?
7. Kodi cholinga chomaliza cha nyimbo zathu za matamando ndi chiyani?
8. Molingana ndi nyimbo za mu Baibulo, ikani mndandanda wa njira zitatu wakuti nyimbo ziyenera kuyankhula ndi magulu osiyansiyana.
9. Kodi Akolose 3:16 akuphunzitsa chiyani pa zakufunikira kwa nyimbo za kulambira?
10. Lembani Akolose 3:15-17 kuchokera pakuloweza.

PHUNZIRO 7

MALEMBA NDI PEMPHERO MU KULAMBIRA

ZOLINGA ZA PHUNZIRO

1. Kuwona kufunikira kwa Malemba mu Kulambira.
2. Kudziwa ndondomeko zogwiritsa ntchito malemba pa kulambira.
3. Kuzindikira kulalikira ngati mbali imodzi ya Kulambira.
4. Kuwona kufunikira kwa pemphero mu Kulambira.
5. Kutsogolera mpingo mu pemphero la mgwirizano.
6. Kumvetsetsa kuti kutenga chopereka ndi mchitidwe wa kulambira.
7. Kupanga mwambo wa mgonero wa Ambuye ngati mwambo wachisagalalo komanso wachisoni.

KUKONZEKERA PHUNZIRO ILI

Lowezani Mateyu 6:5-8.

CHIYAMBI

Mpingo wakutiwakuti ndi wodziwika ndi nthawi yake ya kulambira. Mapemphero awo amatsata ndondomeko iyi:

- Mawu otsekulira kenako zolengeza
- Nthawi ya kulambira (nyimbo za matamando) mphindi 30
- Chopereka/nyimbo za padera/pemphero mphindi 15
- Uthenga mphindi 30
- Nthawi ya kulambira (nyimbo za matamando) mphindi 15

Anthu amakonda nyimbo ku mpingo wa wakutiwakuti. Alendo amayamikira mapemphero amphamvu. Komabe, Abusa a Bill ndi okhudzidwa ndi zotsatira zatsogolo la utumiki wawo. Anthu obadwa mwatsopano akukhamukira kumipingo ina. Kuposera apo, zotsatira za kafukufuku zikuwonetsa kuti anthu amene akhala akupitako kwa nthawi yayitali apeza kuti mpingo, "sukupanga ophunzira a Yesu Khristu okhazikika. Kuchuluka kwa anthu eya; ophunzira, ayi."[59]

Bill akukhulupirira kuti gawo limodzi la vuto ndi kumvetsetsa kwa kulambira. Pa mpingo wa wakutiwakuti, *kulambira* kumafanana *nyimbo*. Abusa a Bill akuyamba kufunsa, "Kodi kulambira kowona kumakhala ndi kuposa kuyimba?" Kodi tikusiyanitsa Mawu a Mulungu ndi pemphero ku kulambira?" Kodi izi zikucheptsa mphamvu ya kulalikira?

» Chonde chitanipo kanthu pa nkhawa za abusa a Bill. Kodi pali kusiyana pakati pa kulambira ndi kulalikira? Kodi mpingo wa wakutiwakuti ungalumikize motani magawo onse a mwambo wakulambira m'malingaliro a wolambira?

KUFUNIKIRA KWA MALEMBA MU KULAMBIRA

Ngati olalikira uthenga timaphunzitsa kuti ziphunzitso zathu ndi kulambira ndi zotsogozedwa ndi Malemba. Timakhulupirira kuti Baibulo likhale phata lalikuli mu kulambira kwathu. Mulungu amayankhula kwa anthu ake mu kuwerenga kwa Mawu. Kuyambira mu nthawi ya Chipangano Chakale, Malemba akhala chikatikati cha kulambira.

Mwachisoni, ngakhale kuti timanena kuti Baibulo ndi tsinde la kulambira kwathu, mipingo yambiri imakhala ndi malemba ochepa m'mapemphero awo. Ndizotheka kukhala nawo ku mapemphero ku mipingo ndikumva malemba ochepa kwambiri akutchulidwa. Izi zili kutali ndi kulambira kwa Baibulo.

Kuwerenga Mawu Kunali Kofunikira Mu Kulambira kwa Baibulo

» Werengani Eksodo 24:1-12.

Pa Eksodo 24:7, Mose anatenga Buku la pangano, ndipo anawerenga mmakutu a anthu onse. Anthu analonjeza kutsata malamulo a Mulungu: "Zonse zimene Yehova wanena tamva, ndipo tidzachita." Patatha izi, Mulungu analemba malamulo moumba mkota (Malamulo Khumi) pa magome a miyala. Israeli anali anthu a Bukulo. Malamulo olembedwa anali chikatikati cha kulambira kwa Israeli.

59 Izi zatengedwa kuchoka kukafukufuku amene anachitika ndi umodzi mwa mipingo ikuluikulu ku America. Anapeza kuti mwa anthu awo otembenuka mtima sanafike pa kukhala ophunzira enieni.

Mawu a Mulungu anali chikatikati cha Chihema komanso Kachisi. Madyerero a pachaka anali ofunikira mu chaka cha chi Yuda. Pa Paska, madyerero a Zipatso Zoyamba kucha, madyerero a Misasa gawo la Mawu a Mulungu linawerengedwa kwa pa gulu. Pa zaka zisanu ndi ziwiri zilizonse, mtundu umakumana kudzamvera lamulo likuwerengedwa, ndipo pangano limakonzedwanso.[60]

Mu Chipangano Chatsopano, Paulo analamulira Akhristu kuwerenga malemba pagulu. Izi zinaphatikizirapo Chipangano Chakale, makalata a Paulo ndi zolemba zina zimene zinaikidwa kukhala malemba opatulika.[61] Analingiza mtumiki wachichepere kuti adzipereke yekha kukuwerenga mawu, kulimbikitsa ndi kuphunzitsa (1 Timoteyo 4:13). Mawu a Mulungu anali chikatikati cha kulambira kwa Chipangano Chatsopano.

Kulalikira Mawu Kunali Kofunikira mu Kulambira kwa Baibulo

» Werengani Nehemiya 8:1-18.

Atabwerera kuchoka ku Ukapolo, Ezara anawerenga Chilamulo kwa anthu. Anthu anasonkhana kudzamvera Ezara akuwerenga Chilamulo pamaso pa amuna ndi akazi, ndi iwo amene akanatha kumva; ndipo makutu a anthu onse anatchera kumva buku la chilamulo (Nehemiya 8:3). Ndipo anthu anse pakuvomereza ananena kuti "Ameni" nagwa nkhope zawo mu kulambira. Pamena Ezara ndiomuthangatira anawerenga, analonogosolera malemba napangitsa iwo akumva kuti amvetse kuwerengako. Ichi ndi chitsanso cha kalalikidwe ka baibulo, kulongosolera komanso kupangitsa kuti Mawu a Mulungu afikire kuzosowa za anthu. Kulalikira kwenikweni kochoka mu Baibulo kumapangitsa kulambira ngati zotsatira za Mawu.

Pa Kulalikira kwa Baibulo

"Dalitso la kulalikira kwa Baibulo kowona ndi mtima owala, osati mutu wa ziyangoyango."

Warren Wiersbe

Yesu anafika ku sunagoge tsiku la Sabata monga mwachikhalidwe chake ndipo anawerenga kuchoka mu buku la Yesaya. Atatha Yesu analakira uthenga umene unawonetsera kuti anabwera kudzakwaniritsa lonjezano la Yesaya (Luka 4:16-29).

Mu uthenga wake pa tsiku la Pentekoste, Petro anawonetsera kuti malonjezano a Chipangano Chakale anakwaniritsidwa mu utumiki wa Yesu, ndi kubwera kwake kwa Mzimu Woyera. Anamaliza kufotokozera kwake kwa malemba ndi kuitanira anthu kukulapa ndi kubatizidwa

60 Timothy J. Ralston, "Scripture in Worship" in *Authentic Worship*. Edited by Herbert Bateman. (Grand Rapids: Kregel, 2002), 201.

61 1 Timoteyo 4:13; 1 Atesalonika 5:27; Akolose 4:16; 2 Petulo 3:16.

(Machitidwe 2:14-41). Kulalikira kwa Baibulo kumaitanira anthu akumvawo kuti achitepo kanthu. Kulalikira kumayakhula ku malingaliro a munthu komanso kukuyenera kuyankhula ku mtima. Kulalikira kukuyenera kuti munthu achitepo kanthu kuchokera mu malingaliro. Pamene Yesu sanatsegula Malemba panjira ya ku Emau, mitima yaiwo akumva inagunda mkati mwawo (Luka 24:32).

Kulalikira kunali kofunikira kukufalikira kwa mpingo oyamba. Mu Machitidwe, Mawu a Mulungu akutchulidwa ma ulendo oposa makumi awiri. Atumwi analalikira Mawu a Ambuye; anayankhula Mawu a Mulungu ndi kulimbika mtima konse, anaphunzitsa Mawu a Mulungu. Zotsatira zake, anthu ambiri analandira Mawu a Mulungu; Mawu a Mulungu anakula ndi kuchulukana, Mawu a Mulungu anapambana, ndipo a Mitundu analemekeza Mawu a Ambuye. Mawu a Mulungu anali maziko a uthenga wa Atumwi.

Pamene kulalikira sinjira yokhayo imene malemba amayakhulira, koma ndi njira yoyambirira yobweretsera Mawu a Mulungu kwa anthu a Mulungu. Kuti akwanitse cholinga ichi, M'busa asaiwale kuti Mawu a Mulungu ndiye chikatikati. Kulalikira kwa Baibulo kuzichokera mu Baibulo, kuzifotokozera Mawu ndi kuitanira anthu kukuchitapo kanthu pa Mawu a Mulungu.

Kulalikira Mawu kunali kofunikira mu Mbiri ya Mpingo

Kulalikira kunali kofunikira mu zaka za mazana oyambirira a Mpingo. Mu zaka za mazana awiri Justin Martyr analemba kuti Akhristu amakumana la Mulungu kuti awerenge mabuku a makalata ndi aneneri kuti amve akufotokozeredwa. Pakufika zaka za mazana atatu ndime iliyonse ya ndime zikuluzikulu za Baibulo zimaweregedwa pa nthawi ya kulambira.

Mu nthawi ya zaka zapakatikati, Mpingo wa Katolika unachepetsa ntchito ya ulaliki, Osintha zinthu anabwezeretsa kulalikira pa malo ake mu kulambira. Cholinga chakusintha kwa kalalikidwe sikunali ku sangalatsa anthu, kufikira zolinga olalikirawo, kapena kufikira zofuna za chikhalidwe cha kudera. Cholinga cha kulalikira chinali kusanthula Mawu a Mulungu mosamalitsa kwambiri; kufotokozera malemba munjira yoti ibweretse kusintha kwa omvera ndi kupangitsa kusintha kwa moyo.

KUPANGA MALEMBA KUKHALA CHIKATIKATI CHA KULAMBIRA

Ngati Malemba akuyenera kukhala chikatikati mu kulambira kwathu, tingachite motani mfundo iyi? Ndondomeko za mmene tingapangire malemba kukhala chikatikati cha kulambira ndi izi:

Malemba Ayenera Kuikidwa mu Magawo Onse a Kulambira

Tisayembekezere mpakana nthawi ya uthenga kuti timve malemba mu kulambira. Palibe njira ina yabwino yoposa imene tingayambire kulambira koposa kuyamba ndi Mawu a Mulungu.

Lingalirani mipata iwiri ya kulambira. Kodi ndi uti umene ungakhale ndi kuthekera koitanira anthu mkupezeka kwa Mulungu?

1. "Zikomo chifukwa chobwera ku tchalichi lero. Mvula inapangitsa kuyenda kukhala kovuta kwa ena mwa inu, koma ndili okondwa kuti munabwera. Tiyeni tiyike chidwi chathu pa Mulungu ndi kulambira. Kodi mungayimilire pamene tikuyimba 'Woyera, Woyera, Woyera?'"

2. "'Ndinasangalala mmene ananena nane, tiyeni kunyumba ya YEHOVA!' Takulandirani kunyumba ya Mulungu! M'kachisi Yesaya anawona Ambuye okwezedwa pamwamba. Anamva Angelo akuyimba, Woyera, Woyera, Woyera ndi Ambuye wa makamu, dziko lonse ndi lodzala ndi ulemero wake.' Tiyeni pomodzi tiyimbe matamando, 'Woyera, Woyera, Woyera.'"

Otsogolera oyamba anatikumbutsa za mavuto amayendwe, otsogolera wachiwiri anatikumbutsa za Chimwemwe cha kulambira. Otsogolera oyamba anayamba ndi mawu awamba, otsogolera wachiwiri anayamba ndi Mawu a Mulungu. Otsogolera oyamba analengeza nyimbo ya wamba; otsogolera wachiwiri, anatikumbutsa kuti angelo amaimba nyimbo iyi mu kutamanda kwawo kwa Mulungu. Kodi ndi mpingo uti umene uyimbe ndi mphamvu?

Zitachitika za pa September 11, 2001, chifwamba cha zigawenga ku United States, mipingo inasonkhana m'matchalitchi mwawo pa Sabata kuti akalambire monga mwachizolowezi. Fananizani kutsegula kwa mapemphero a mipingo iwiri iyi.

1. "Zikomo pokhala nafe tsiku la lero. Sabata ino yakhala yovuta kwambiri mu dziko lathu. Ambiri a ife tili pa chisoni. Zikomo chifukwa chobwera kudzapembedza ngakhale kuti nthawiyi ndiyowawa kwambiri. Tiyamba ndi kuyimba 'Mtandawo Wakale.'"

2. "Mulungu ndiye pothawirapo pathu, ndi mphamvu yathu, thandizo lopezekeratu munsautso. Munyengo zovutazi tisaiwale kuti Iye ndiye chiyembekezo chathu; pothawirapo pathu. Tiyeni tilumikizane limodzi pamene tikukumbukira kuti, 'nangula wathu wamphamvu ndi Mulungu wathu, Chikopa **wosalephera**."

Wotsogolera woyamba anawakumbutsa zachisoni chawo; wotsogolera wachiwiri anawakumbutsa zoti Mulungu ndiye chiyembekezo chawo. Malemba ndi nyimbo

mokhudzana ndi malembawo inapereka madziko olimba mu sabata imene chiyemebekezo cha anthu chimayesedwa.

Malemba akhoza kugwiritsidwa ntchito magawo ambiri mu msonkhano wa kulambira:

- Mawu otsegulira mwambo wa mapemphero
- Kuitanira ku chopereka
- Mawu a nyimbo
- Pemphero

Kulambira kwathu kuyenera kukhale kodzala ndi Mawu Mulungu. Kulambira ndi kuvomerezana ndi vumbulutso la Mulungu Iye mwini mu Mawu ake. Malemba apezeke pa madera onse a mwambo wa kulambira.

Kuwerenga kwa Malemba Kukhale ndi Malo Aakulu mu Kulambira

Kodi munayamba mwamvapo m'busa akunena kuti, "Tilibe nthawi yambiri lero ndipo ndili ndi uthenga wautali, ndiye ndidumpha kuwerenga kwa Mawu?" Kodi chofunikira kwambiri ndi chiyani, Mawu a Mulungu ndi mawu athu? Tikuyenera kupereka mpata ku malemba mu nthawi ya kulambira.

Chifukwa chakuti kuwerenga malemba ndi kulambira, tikuyenera kukhala ndi tcheru mmene timawerengera. Ayenera kuwerengedwa momveka ndi mwa ulemu. Owerenga (kaya ndi m'busa kaya ndi munthu wamba) akonzekere mapemphero asanyambe. Muzaka za mazana atatu zoyambirira za mpingo, udindo wa owerenga malemba unali wopatulika. Owerenga anali kusunga mabuku amene apatsidwa kuti akawerenge kunyumba ndikumaphunzira kuwerenga. Akamawerenga mu mwambo wa kulambira, amakhala okonzeka kuwerenga momveka ndi momveka bwino.[62]

Kumbukirani kuti awa ndi Mawu a Mulungu akuwerengedwa munyumba ya Mulungu kupita kwa anthu a Mulungu ngati mchitidwe wa kulambira. Ngati nyimbo zamatamando zimafunika kukonzekera, Mawu a Mulungu amafunika kukonzekera. Sikunyadira mukuthekera kwathu; koma ndikuwonetsetsa kuti Mawu a Mulungu akufikiradi kwa omvetsera. Awa ndi Mawu a Mulungu; ndi ofunikira!

Tipangitse kuwerenga kukhala kwa tanthauzo. Kugwiritsa ntchito njira zosiyana zakawerengedwe kudzapangitsa malemba kukhala a chilendo kwa omvera.

1. **Nthawi zina malemba akhoza kuwerengedwa ndi otsogolera pamene mpingo ukumamva Mulungu akuyankhula.** Mtundu uwu wa kawerengedwe ndi ogwirizana ndi mabuku Asanu a Mose komanso mabuku ambiri a aneneri.

62 Keith Drury, *The Wonder of Worship*, (Fishers, IN: Wesleyan Publishing House, 2002), 35.

2. Nthawi zina otsogolera ndi mpingo akhoza kumasinthana kuwerenga kumeneku. Ambiri mwa Masalimo ndi ogwirizana ndi mtundu uwu wa kuwerenga kovomereza.

» Werengani Masalimo 136. Mtsogoleri wa kalasi ayambe vesi; kalasi iyankhire, "pakuti chikodi chake n'chonsatha."

Chiphunzitso cha paphiri ndi chothekanso kuwerenga molandizana (Mateyu 5:1-10):

Otsogolera: Odala ali osauka muuzimu,
Mpingo: chifukwa wawo uli ufumu wa kumwamba.
Otsogolera: Odala ali akulira,
Mpingo: chifukwa adzatonthodzedwa.

3. Malemba ena akhoza kuwerengedwa ndi mpingo mogwirizana pamodzi. Ngati nyimbo ya mpingo wonse, kuwerenga malemba ngati thupi kumaonetsera umodzi wa mpingo. Mpingo wonse pamodzi kugwirizana kuwerenga Mawu a Mulungu. Mapemphero ngati Masalimo 124 ndi oyenera kuwerenga mogwirizana pamodzi.

Nkhani ya Nehemiya pa zakuwerenga chilamulo kwa Ezara ikuwonetsa mphamvu pamene malemba ndi chimake cha kulambira kwathu.

» Werengani Nehemiya 8 mobwereza ngati mukufuna kuti muonenso nkhani imeneyi.

Zindikirani ndondomeko za kuwerenga.

- Ezara anatsegula buku pamaso pa anthu onse. Panali kulumikizana kwa zimene amaona ndi Mawu.
- Anaima pamwamba pa anthu onse. Owerengayo amatha kuwonekera bwinobwino ndi kumveka.
- Akayamba kuwerenga, anthu onse amaimirira. Panali kuchitapo kanthu kwa Mawu kowoneka.
- Akamawerenga, anthu onse anayankha, "Ameni, Ameni," kukweza manja awo, nawelamitsa mitu yawo pansi ndikulambira Ambuye ndi nkhope zoloza pansi. Amawonetsera kugonjera kwawo ku Mawu a Mulungu.
- A Levi amawerenga chilamulo cha Mulungu momveka bwino, ndipo anapereka tanthauzo, kuti anthu amvetsetse kuwerengako. Anapereka chidwi kukumvetsa Mawu a Mulungu. Ichi ndi cholinga cha kulalikira lero.
- Anthu analira, pamene anamva mawu a chilamulo. Nehemiya anawalamulira kuti akondwere, "pakuti chimwemwe cha YEHOVA ndiye mphamvu yanu." Mawu a Mulungu analimbikitsa kulapa komanso kukondwera.

Ngakhale kuti china chilichonse cha mwambo wapadera uwu sichidzabwerezedwa m'mapemphero mwathu, nkhani iyi ikuwonetsa mphamvu ya malemba. Tiyenera kupanga malemba kukhala chimake cha kulambira kwathu.

FUFUZANI

Kodi mpingo wanu umadziwa kufunikira kwa kuwerenga Baibulo mkati mwa mapemphero? Longosolani zikhalidwe zina ndi machitidwe ena amene mumawawona mu mpingo panthawi ya kuwerenga Mawu.

Pa mulingo wa Sabata, kodi ndi ndime zosiyana zingati za malemba zimene zimamveka ku mpingo wanu? Kodi wolambira amadziwa chifukwa chimene ndime ina iliyonse yaphatikizidwapo?

Kulalikira kwa Mawu Kukhale Chimake cha Kulambira Kwathu

Monga kayimbidwe ka nyimbo kamasintha mu m'badwo uliwonse, kalalikidwenso kamasintha kuti kafikire zosowa za m'badwo ulionse. Malemba sakufotokozera mtundu umodzi wa kaimbidwe *ngati* Kayimbidwe ka Baibulo ka nyimbo za matamando; malemba safotokozera njira imodzi ya kalalikidwe *ngati* kalalikidwe ka Baibulo.

Kachitiwe kakhoza kusintha kuchokera ku m'badwo wina kupita ku m'badwo wina, komanso kuchokera ku chikhalidwe china kupita ku chikhalidwe china; koma zenizeninzo sizisintha. Momwemonso, kalalikidwe kakhoza kusintha kuchokera ku m'badwo wina kupita ku m'badwo wina koma zenizenizo zisasinthe.

Mauthenga m'malemba akuonetsa kuti kulalikira kwa Mawu a Mulungu ndi udindo oyambirira wa mlaliki amene amaima pamaso pa mpingo. Chidwi pa Mawu a Mulungu chikhalebe chokhazikika pakulalikira kwa makono. Kusintha ukadaulo ndi njira za kaphunziridwe kakhoza kusintha kalalikidwe; koma zenizeninzo ziyenera zikhazikike mu malemba.

Kulalikira ngati Kulambira: Zotsatira Zowonekera

Kodi zotsatira zodziwika zosakhala bwino zoona ulaliki ngati kulambira ndi chiyani? Kodi izi zidzakhudza motani mawonedwe athu a ulaliki?

> **"Ngati kulalikira si mchitidwe wa kulambira, ndiye kuti mpingo udzathera pa kulambira mlaliki osati kulambira Mulungu."**
>
> **Warren Wiersbe**

Kulalikira kumafunika kuvomereza kochokera kwa mlaliki.

Ngati kulalikira ndi kulambira, ndife oyenera kukonzekera mosamala. Tiyenera kubweretsa mphatso zabwino pa gome la Mulungu. David sanapereke chimene sichinapangire mtengo waukulu; tisamabweretse mauthenga osakonzekera ngati Mphatso yathu kwa Mulungu. Tikuyenera kukonzekera uthenga wathu mosamalitsa tsiku lamapemphero lisanakwane (2 Samueli 24:24).

Kulalikira kumafunika kuvomereza kuchokera kwa anthu onse.

Ngati kulalikira ndi kulambira, anthu akuyenera ayankhepo. Mukulambira timaona Mulungu, timadziona tokha, ndipo timaona zosowa za dziko lathu (Yesaya 6:1-8; onani Phunziro 1). Mauthenga athu azivumbulutsa Mulungu kwa omvera, mauthenga athu azitsutsa omvera za chosowa, ndipo mauthenga azilimbikitsa mpingo kufikira dziko lotaika. Kulalikira ngati kulambira kudzabweretsa kutsutsika kwa wochimwa ndipo kudzalimbikitsa okhulupirira ku chisokole.

Kulalikira kumafunika kuvomereza kochokera kwa mlaliki.

Ngati kulalikira ndi kulambira, tidzadziwa kuti kulalikira kumafunika kuchitapo kanthu kwathu. Ngati tikonzekera kulalikira ndati m'chitidwe wa kulambira kodzipereka tidzaona Mulungu; tizatsutsika m'madera amoyo wathu amene akusoweka kutsutsika; tidzaona zosowa za dziko lotizungulira. Pakuchitapo kanthu, tidzalira ndi Yesaya, "Ndiri pano; nditumeni." Kulalikira kowona kudzasintha mulaliki. Tisamabweretse unthenga wa Mulungu kufikira Mulungu atayankhula nafe ndipo tidzachitapo kanthu.

> **"Kulalikira ngati sikulambira, ndiye kuti ndikunyoza... Uthenga woona ndi kuchita kwa Mulungu osati kuyankhula chabe kwa munthu."**
>
> **Zatengedwa kuchokera pa zolembedwa za J.I. Packer**

Yesu sanadzudzule alembi (alaliki) anthawi imeneyo chifukwa cha uthenga wawo woyipa; anadzudzula chifukwa cholephera kukhala zomwe iwo amalalikira. Amadziwa malemba komanso matanthauzidwe a Malemba, koma sanali osinthika ndi malemba. Yesu anati, "Koma musachite zimene amachita, popeza sachita zimene amaphunzitsa" (Mateyu 23:3). Ngati kulalikira ndi kulambira, ife ngati abusa tidzasinthika ndi choonadi chimene timalalikira. Zotsatira zake, Mulungu adzayankhula kudzera mwa ife kusintha mitima ndi miyoyo ya anthu amene timawalalikira.

Mlaliki ayenera kupatsidwa mphamvu ndi Mzimu Woyera.

Ngati kulalikira ndi kulambira, mlaliki apatsidwe mphamvu ndi Mzimu Woyera. Monga magawo ena onse akulambira amadalira pa Mzimu Woyera, mlalikinso ayenera adzozedwe ndi Mzimu wa Mulungu kuti akhale wa mphamvu.

» Werengani 2 Akorinto 3:3-18.

Timabweretsa nsembe yathu yabwino ya kukonzekera ku uthenga; komabe kukonzekera kwathu kutatha, mphamvu mu kulalikira imabwera kudzera mwa Mzimu Woyera. Popanda mphamvu ya Mzimu Woyera, tikhoza kuyankhula kumaganizo, kusangalatsa anthu, ndipo tikhoza kukhala ndi mfundo zambwino, koma sitidzasintha miyoyo.

FUFUZANI

Kodi kulalikira kwanu ndi mchitidwe wa kulambira kwa Baibulo? Ngati munthu atati azikumverani mukulalikira pafupi pafupi, kodi adzamva choonadi cha Baibulo chokhazikika?

ZOOPYSA ZA KULAMBIRA: KUSOWA KWA MAWU

Baibulo silikupezanso malo m'moyo watsiku ndi tsiku wa okhulupirira ambiri atsopano. Zachisoni, silikupezanso mu kulambira kwa sabata ndi sabata m'mipingo yambiri. Pamene mpingo oyamba unayimba masalimo, mipingo ina lero imayimba nyimbo zokhala ndi zinthu za Baibulo zochepa kapena kukhaliratu opanda. Pamene mpingo oyamba unawerenga ndime zazitalizitali za malemba, malemba alowedwa mmalo ndi nyimbo komanso uthenga umene umapereka chidwi chochepa ku Mawu a Mulungu.

Atsogoleri ena ambiri akulambira kwa makono amakakamira kuti kuwerenga malemba kwa pagulu sikuyankhula ku zosowa za makono. M'busa odziwika bwino ogwira ntchito

pa mpingo kuti asanthule malalikidwe ake. Anamuuza kuti akugwiritsa ntchito kwambiri Baibulo! "Ndibwino kwa inu kukhazika uthenga wanu pa maziko a Baibulo, koma muyenera kupezanso china choyenera mwamsanga, kapena apo ayi tisiya kumvera." Anthu ogwira ntchito awa sanaganize kuti Baibulo ndilofunikira kwa anthu lero.

Ngati otsogolera matamando, tikuyenera kusunga chikatikati cha malemba pa kulambira. Mukulambira, timayankhula ndi Mulungu kudzera mu pemphero ndi nyimbo za matamando. Mu kulambira timamva Mulungu Mulungu akuyankhula kwa ife kudzera mu kuwerenga komanso kulalikira kwa Mawu. Pakusatengera kalambiridwe kathu, tisamataye chimake cha Mawu a Mulungu mukulambira kwathu.

» Onaninso Nehemiya 8. Pangani mndandanda wa mawu aliwonse amene akuwonetsa kufunikira kumene anthu amaika pakuwerenga kwa Chilamulo. Fananizani kuwerenga uku kwa mawu mu kulambira kwanu kwa lero. Fotokozani njira imodzi yodziwika imene ingaonjezere mphamvu ya malemba mkulambira kwanu.

KUFUNIKIRA KWA PEMPHERO MU KULAMBIRA

Kathy[63] ndi Mkhristu odzipereka. Ngakhale anali pa sukulu, anatenga nthawi ya payekha ndi Mulungu mmamawa uliwonse. Asanalandire chakudya cha mmawa, amakhala ndi nthawi kuwerenga Baibulo ndi kupemphera.

Koma tsopano ndi mayi wa ana anayi, pemphero ndi kuwerenga Baibulo kukukhala kovuta. Mwana wina ndi wakhanda ndipo amamudzutsa Kathy usiku. Kathy amaona kuti kumakhala kovuta kuti adzuke mmamawa ana asanadzuke. Nthawi ya usiku, amawona kuti ndi otopa kuti akhazikike pa pemphero.

Kathy amakhala okondwa tsiku la Mulungu likafika. Tsiku la Mulungu lili lonse, amalandira chilimbikitso munthawi ya kulambira, koma mkati kwa sabata, amafooketsedwa. Amaona kuti moyo wodzipereka wakhala wolephereratu.

» Choonde mpatseni Kathy malangizo amene angamuthandize pamoyo wake odzikhutula.

Tinayamba phunziroli ndi kuwerenga kwa malemba akulambira. Tipitiriza ndi phunziro la pemphero mukulambira. M'malemba, Mulungu amayankhula nafe; mupemphero, timayankha kwa Mulungu. Malemba ndi pemphero zikuyenera zikhale mukulambira.

63 Nkhani ya Kathy yatengedwa kuchokera kwa Keith Drury, *The Wonder of Worship*, (Fishers, IN: Wesleyan Publishing House, 2002), 17.

Pemphero la Pagulu ndi Pemphero lamseri Mukulambira kwa Baibulo

Tawona kuti Buku la Masalimo linali Buku la Nyimbo ku Chipembedzo cha chi Yuda. Komanso linali, "buku la mapemphero" la chipembedzo cha chi Yuda. Masalimo munali mapemphero a kulambira kwa pagulu komanso kupemphera kwa mseri. Kupemphera kwa pa gulu ndi kwa mseri kunali kofunikira ku chipembedzo cha chi Yuda.

Kunyumba, Ayuda okhulupirika amapemphera katatu patsiku (Daniel 6:10).[64] Masalimo ambiri ndi mapemphero amseri. Akhoza kuzindikirika ndi kugwiritsa ntchito kwa **Ine** mmalo mwa **ife** mupemphero. Zitsanzo za masalimo a pemphero:

- Masalimo 18 – Nyimbo yothokoza
- Masalimo 32 – pemphero la chimwemwe cha chikhululuko[65]
- Masalimo 38 – pemphero la kulapa
- Masalimo 41 – pemphero la Chifundo
- Masalimo 51 – pemphero la kulapa
- Masalimo 88 – kulira nthawi ya mavuto
- Masalimo 116 – nyimbo yothokoza chifukwa cha chisamaliro cha Mulungu.

Mukachisi, opembedza onse a Chiyuda anasonkhana pamodzi mupemphero la gulu (2 Mbiri 6). Yesaya anabweretsa uthenga wa Mulungu kwa Yuda; "Nyumba yanga idzatchedwa nyumba ya mapemphero ya anthu a mitundu yonse" (Yesaya 56:7). Utatha ukapolo, mapemphero a mu sunagoge amayamba pa kuwerenga kwa Chilamulo ndi mndandanda wa mapemphero.

Mtundu wakapemphereredwe ka Chihebri unapitirira mumpingo oyamba. Akhristu a zaka zana limodzi zoyambirira amapemphera katatu patsiku kunyumba. Akhristu akakumana kuti apemphere, amapemphera ngati thupi. Pemphero la Ambuye linali mbali imodzi ya mwambo wa mapemphero ena onse amaperekedwa pa mwambo wa mapemphero alionse.

"Akhristu ambiri amakhulupirira mu nthawi yachete ya pawokha kusiyana ndi kukhala nayo."

Keith Drury

Pemphero mu Kulambira Lero

Ngati pemphero linali lofunikira mu kulambira kwa Baibulo, pemphero layenera kukhala lofunikira mu kulambira kwathu lero mapemphero a pagulu ndi amseri onse ndi ofunikira.

64 Chidzolowezi cha Danieli chinali chodziwika pakati pa a Yuda okhulupirika.

65 Salimo ili mwina linapangidwa atangotha kulapa mu Masalimo 51.

Pemphero la mseri limatilumikiza ku Mpesa ndikutipatsa thanzi la moyo wathu wa uzimu. Kusowa pemphero la mseri kukhoza kubweretsa kosowekera kwa mphamvu ya uzimu m'mipingo yambiri. Ngati Yesu anafuna nthawi ya pemphero la mseri pa nthawi ya utumiki wake wa padziko, kuli bwanji ife timadalira motani pa pemphero kuti tikhale ndi moyo wathanzi wa uzimu komanso mphamvu mu utumiki.

Pemphero la pagulu ndi chinthu chofunikira cha kulambira. Mipingo ina imaika chidwi chochepa ku pemphero. M'busa wina anateteza kusowa kwa pemphero la gulu mu mpingo mwake ponena kuti; "Sungasagalatse anthu pamene maso awo ali chitsekere."[66] Anakhulupirira kuti kusangalatsa anthu ndi kofunikira kwambiri kuposa kusangalatsa Mulungu.

Pemphero la mgwirizano limakonza maganizo olakwika oti chi Khristu chimakhuza ine ndekha ndi chiyanjano changa ndi Mulungu; ife ndi chiwalo chimodzi cha thupi. Pamene tikumva zopempha zam'pemphero ndi kukhala limodzi mpemphero, timazindikira matenda a Khristu amzathu, kukhumudwa kwawo komanso zinthu zowachitikira m'moyo. Pemphero la mgwirizano limatikumbutsa kuti Mulungu amasamala mpingo ngati thupi.

Monga malemba ayenera kugwiritsidwa ntchito mu msonkhano wa chipembedzo, pempheronso liperekedwe mu msonkhano wa mapemphero onse. Kuyambira ku pemphero lotsekulira limene limaitanira kupezeka kwa Mulungu mu msonkhano, kufikira ku nthawi yokhazikika yopempherera zosowa za anthu, mpaka ku pemphero la mdalitso potseka pamene anthu akupita kukatumikira kudziko, pemphero likhazikike pa kulambira kwathu.

KUPANGA PEMPHERO KUKHALA CHIMAKE CHA KULAMBIRA

Kodi ndi njira zina ziti zodziwika zimene zingapange pemphero kukhala mbali yofunikira ya kulambira kwa gulu? Apa pali ziganizo zisanu ndi chimodzi.

Khazikitsani Moyo Wanu Wa Pemphero la Mseri

Palibe munthu angakhale okonzeka kutsogolera chipembedzo mpaka iye atayamba kulambira payekha. Palibe munthu angakhale okonzeka kutsogolera ma pemphero a pagulu asanapemphere payekha mseri. Pokhapo pamene taumba moyo wa pemphero la mseri ndi pamene tikhala

"Chinthu chofunikira kwambiri pa moyo wa Chikhristu ndi kulambira kwa tsiku ndi tsiku ndi kuyamika Mulungu ngati maziko akukhala kwathu ndi moyo."

Dennis Kinlaw

66 Zatengedwa kuchokera mwa Keith Drury, *The Wonder of Worship*, (Fishers, IN: Wesleyan Publishing House, 2002), 28.

okonzeka kutsogolera mapemphero a pagulu. Ngati otsogolera matamando, dziperekeni podzidzoloweza tsiku ndi tsiku ku mapemphero a pawekha.

Phunzirani Kupemphera

Ophunzira a Yesu anapempha, "Tiphunzitseni ife kupemphera" (Luka 11:1). Poyankha, Yesu anaphunzitsa chitsanzo cha pemphero lotchedwa Pemphero la Atate. Pemphero likhoza kuphunziridwa.

Mugawo lina, pemphero ndichikhalidwe cha mwana wa Mulungu, komabe, pemphero likhoza kuphunziridwa. Mwana wa ng'ono amaphunzira kulankhula popanda kulowa mkalasi ya kalankhulidwe. Komabe, pamene mwana akula, amaphunzira zamburi zokhunza chilankhulo, mawu komanso kulankhula kwabwino. Momwemonso, mkhristu wang'ono amagoyamba kufuna kuyankhula ndi Mulungu, koma pemene tikukula mu chi khulupiriro, kumvetsa ndi kudziwa kwa pemphero kumakhala kozama.

Mabuku a pemphero akhoza kuzamitsa kumvetsetsa kwanu kwa pemphero. Mabuku ena apamwamba amene angapindulire Mkhristu aliyense ndi awa:

- *Power Through Prayer* by E.M. Bounds
- *With Christ in the School of Prayer* by Andrew Murray
- *Mighty Prevailing Prayer* by Wesley Duewel

Pempherani Mawu a Malemba

Palibe malo ena abwino amene mungaphunzire pemphero kuposera m'malemba. Suluku yoyamba ya pemphero ndi Baibulo. Masalimo ndi mabuku ena a pemphero mu baibulo amatiphunzitsa kupemphera mwa mphamvu. Mumbiri ya Mpingo, akuluakulu m'chiKhristu adagwiritsa ntchto malemba popemphera. Ena mwa Mapemhero apamwamba mu Baibulo ndi awa:

- ***Pemphero la Kukonda***. Eksodo 15:1-18, 1 Samueli 2:1-10, 1 Mbiri 29:11-20, Luka 1:46-55, Luka 1:68-79, 1 Tomoteo 6:15-16, ndi Chivumbulutso 4:8-5:14.
- ***Pemphero la Kuvomereza Kulakwa.*** Ezara 9:5-15, Masalimo 51, ndi Danieli 9:4-19.
- ***Pemphero lo Pembedzera.*** Genesis 18:23-33, Eksodo 32:11-14, Aefeso 1:15-23, ndi Afilipi 1:9-11.

Khazikikani pa Kuyanjana ndi Mulungu

Nthawi zambiri, mapemphero amangobweretsa zopempha zokhazokha kwa Mulungu. Anthu ena amabweretsa mndandanda wa zopempha, kumuthikoza chufufukwa choyankha

mapemphero adzulo, kunako mkunena ku "Ameni." Pemphero lenileni leni likuyenera lisangokhala la zopempha zokha zokha; pemphero ndi chiyanjano ndi Mulungu.

Pemphero la Atate likupereka chitsanzo cha pemohero (Mateyu 6:9-13). Pemphero la Atate muli:

- **Kukonda**: "Atate wathu muli kumwamba, dzina lanu liyeretsedwe."
- **Kugonja**: "Ufumu wanu uze, kufuna kwanu kuchitidwe, monga ku mwamba chomwecho pansi pano."
- **Kupempha**: "Mutipatse ife chakudya chanthu cha laro."
- **Kulapa**: "Ndipo mutikhululukire ife mangawa athu, monga ife tiakhululukira amangawa athu."
- **Pemphero la Chitsogozo**: "Musatitengere ife kokatiyesa, koma mutipulumutse kwa oyipawo."
- **Kutamanda**: "Pakuti wanu uli ufumu ndi mphamvu ndi ulemerero kwa nthawi zonse. Amen."

Akhristu ambiri amatsatira chitsanzo cha pemphero la Yesu cha magawo anayi; Kukonda, kulapa, kuthokoza, ndi kupempha.

Kukonda

Pemphero lisadumphe kulemekeza ndi kutamanda. Pakuyamba ndi kuyamika, timaonetsetsa kuti pemphero lathu ndi lofunikira kuposa mndandanda wa zopempha zathu zofuna thandinzo. Masalimo amapereka chitsanzo cha pemphero limene limene lili lokhazikika mu matamando. Ngakhale masalimo olira amakhala ndi matamando. Ngati pemphero ndi kulambira koona, lidzakhala ndi kulemekeza Mulungu.

Kulapa

Yesaya 6 akuwonetsa tikamuona Mulungu (kumukonda), tidziwona tokha. Tikadziwona tokha mkuunika kwa chiyero cha ngwiro cha Mulungu, timvetsa kufunikira kwathu kwa kulapa. Palibe mkhristu, mosasamala kuti ngokhwima bwanji muuzimu, mosasamala amalankhula bwanji mozama ndi Mulungu, angafike pa mulingo onena kuti, "sindikusoweka kulapa, ndine wagwiro." Yesu anati kwa Ophunzira ake, "Pamene mupemphera, munene kuti… ndipo mutikhulukire machimo athu; pamene tikhululukira akutichimwira" (Luka 11:4) Ku pembedza koona kumayenda pamodzi kulapa.

Kuthokoza

Kukonda kumamukweza Mulungu pa chimene ali, Kuthokoza kumamukweza Mulungu pachimene akupanga ku dziko lathu. Kuthokoza kumabweretsa kuzindikira kuti mphatso iliyonse yabwino imachoka ku mwamba (Yakobo 1:17). Mukuthokoza, timathokoza Mulungu

pachimene wachita m'moyo mwathu. Nkhani ya akhate Khumi ikuwonetsa kufunikira kwa kuthokoza (Luka17:12-19).

Kupempha

Mupemphero la Atate, Yesu anawonetsa kuti Mulungu amaikapo chidwi pa zopempha ana ake. Mulungu sali ngati olamulira wa dziko lapansi amene amakhala otanganidwa kuvutitsidwa ndi zosowa za anthu ake. Komatu Mulungu ndi Atate wangwiro amenena amakondwera kupereka mphatso zabwino kwa ana ake. Mu pemohero Atate, tikulimbikitsidwa kupempherera zopempherera za wamba ("Mutipatse ife chakudya chathu cha lero") ndi chitsogozo cha uzimu ("musatitengere ife kokatiyesa").

Mupemphero la Atate, timaphunzira kugongera ku chifuniro cha Mulungu tikapempha. Monga ana odalira, timaphunzira kuti chifuniro chake nde ndi changwiro; "Ayi" wake ndiwotichitira ife ubwino. Pemphero chinthu chomuopysezera Mulungu kuti achite zofuna zathu. Pemohero ndi chizolowezi cha uzimu chimene chimatibweretsa ife kukugonjera mwa chimwemwe ku chifuniro cha Mulungu.

Lumikizitsani Zofuna Zanu ndi za Mulungu

Pemphero limatiwonetsa chimene chiri chofunikira kwambiri kwa ife. Kodi Chimene chimapatsa mphamvu pemphero lathu lowona mtima ndi zosowa zathu za kuthupi kapena zosowa zathu za kuuzimu?

Paulo powapempherera a Khristu Atesalonika, anati, "timakupemphererani nthawi zonse, kuti Mulungu wathu akuoangeni kukhala oyenera maitanidwe ake, kuti mukakwaniritse tchito iliyonse yabwino, ndi tchito iliyonse ya chikhulupiriro mu mphamvu yake, kuti dzina la Ambuye wathu limekezedwe mwainu, ndi inu mwa Iye…" (2 Atesalonika 1:11-12). Kukhuzika kwakukulu kwa Paulo kunali koti Mulungu akwaniritse cholinga chake mu miyoyo yawo. Akhristu awa anali akuzunzika, koma pemphero la Paulo silinali Mulungu awapulumutse ku chizunzo chawo. Malo mwake anapemphera kuti dzina la Ambuye Yesu limemekezedwe.

Monga zopempha zathu zimaonetsa zinthu zomwe timaika patsogolo, kuthokoza kumaonetsa zinthu zathu zofunikira poyambirira. Ngati kuthokoza kwathu kungakhale kwa madalitso akuthupi, ndiye kuti madalitso akuthupi ndi amene timaika patsogolo. Ngati kuthokoza kwathu mkokhuza thandinzo la Mulungu m'moyo wathu wa uzimu, ndiye kuti kukula moyo wa uzimu ndiumene timaika pa tsogolo.

Paulo mu pemphero lake la kwa Atesalonika, anayamika Mulungu chifukwa cha chikhulupiriro cha anthuwo chinali kupitirirabe kukulirako, komanso chikondi cha pa abale chinalinso kukulirako (2 Atesalonika 1:3). Chiyamiko chake chachikulu sichinali pa madalitso a kanthawi; koma chiyamiko chake chachikulu chinali pakukula kwao mu

mzimu. Kodi chimene chimakupangitsani kuti mupereke chiyamiko chachikulu, madalitso andalama kapena umboni woonetsa kukula kwa uzimu mumoyo wanu?

Yankhulani ndi Mulungu, osati Mpingo

Kupyolera mumalemba, Mulungu amalankhula ndi mpingo. Mupemphero, mpingo umalankhula ndi Mulungu. Pa nthawi yopemphera pamodzi ngati gulu, sinthawi yoti wotsogolera popemphera pamenepo apezepo mwayi wakuuza anthuwo zimene iye akufuna! Pemphero limalankhula kwa Mulungu. Pemphero limalankhula kwa Mulungu.

Yesu anawauza ophunzira ake mmene anagapempherere mumzimu wa kulambira koona:

> Ndipo pamene mupemphera, musakhale ngati onyenga. Pakuti amakonda kuimirira ndi kupemphera makachisi, m'misewu, kuti awonedwe ndi anthu. Indetu, ndinena kwa inu, alandira kale mphotho yawo. Koma pamene mupemphera lowa mchipinda chako nutseke chitseko ndi kupemphera kwa Atate wako wa mseri. Ndipo Atate wako wakuona mseri azakuoatsa iwe mphoto. Ndipo pamene mupemphera musamabwerereze-bwereze monga Amitundu amachitira, pakuti aganiza kuti amvedwa mwakuchuluka kwa mawu awo. Usakhale ngati iwo, pakuti Atate wako adziwa zomwe usowa usanapemphe (Mateyu 6:5-8).

Pemphero lenileni siliyesera kumukopa Mulungu kapena mpingo; limayankhula mwachindunji ndi momveka bwino kwa Atate wathu wa kumwamba.

» Kodi mungachite chiyani kuti moyo wanu wa panokha wa pemphero ukule? Kodi mungapange bwanji kuti ma pemphero a pagulu akhale atanthauzo mu tchalichi?

CHOPEREKA NGATI KUVOMERA MAWU A MULUNGU

Pemphero ndikuyankhapo ku mawu a Mulungu. Chifukwa cha ichi, tikuyenera kutsatira kuwerenga kwa mawu, ndi uthenga ndi pemphero. Mupemphero, timavomera ku choonadi chomwe takandira ku chokera ku Mawu a Mulungu; timadzipereka tokha ku kukumvera.

Choperekanso ndi kuvomera ku Mawu a Mulungu. Mu Chipangano Chakale, nsembe (chopereka) inali kuyankhapo kwa wolambira ku chilamulo (Mawu a Mulungu). Mu Chipangano Chatsopano, chopereka chikuimirira kudzipereka kwa moyo wathu wonse kwa Mulungu.

Chopereka ndi gawo limodzi la chipembedzo. Wolemba masalimo anaitanira wolambira kuti abweretse chopereka m'mabwalo ake (Masalimo 96:8). Olemba Ahebri analumikiza kulambira ndi kupereka; "Musaleke kuchita zabwino kupereka chomwe mulinacho, pakuti nsembe zotere zisangalatsa Mulungu" (Ahebri 13:16). Paulo anawuza Afilipi kuti chopereka

chawo chinali nsembe ya fungo labwino, nsembe yolandirika ndi yokondweretsa Mulungu (Afilipi 4:18).

Chikhulupiriro cha Kupereka kwa Kulambira

Anthu ambiri angopita ku tchalichi, amaona ngati chopereka ndi chingofikira zosawa za pa mpingo. Izi zimapangitsa kuti chopereka chikhale chongosinthana ndalama osati chochitika cha uzimu mukulambira. Udindo wa Khristu udziwike ngati gawo lakulambira. Mfundo iriyonse mwa mfundo zotsatirazi ikhale muchiphunzitso chakupereka kochoka mu baibulo.

Kupereka kokhala ndi kulambira kumalimbikitsidwa ndi chisomo osati mantha.

Kupereka ngati chochitika cha kulambira mwa kuthokoza chisomo cha Mulungu. Paulo anapempha a Korinto kuti apereke kuthandizira a Khristu aku Yerusalemu. Sanawawopyeze kuti, “Inu *muyenera* kupereka chifukwa tsiku lina muzafuna thandizo.” Koma mmalo mwake anamaliza pempho lake ndi kuamika, “Mayamiko apite kwa Mulungu chifukwa cha mphatso yake yosatheka kuneneka!” (2 Akorinto 9:15). Kupereka kwawo kunatakatsidwa ndi kuthokoza chifukwa cha mphatso ya chisomo. Ngati kupereka ndi kupembedza kuyenera, kumachokera ku mtima ofuna.

Kupereka kokhala ndi kulambira kumatakasidwa ndi chikondi osati mphoto.

Kulambira kowona kumatakatsidwa ndi **chikondi cha pa Mulungu**, osati pokhumba mphoto. Mphatso za ndalama ndi chithuzithuzi cha mphatso yathu kwa Mulungu. Paulo adayamikira a khristu aku Masedonia chifukwa “anazipereka okha koyamba kwa Ambuye kenako mwachifuniro cha Mulungu kwa ife” (2 Akorinto 8:5). Mphatso zawo zimaimirira chikondi chawo cha pa Mulungu ndi pa Atumwi amene anabweretsa uthenga uthenga wabwino mdera lawo.

Monga nyimbo kapena chichitika china chirichonse cha kulambira zikhoza kuchitika pa zifukwa zolakwika, kupereka kukhoza kutakatsidwa kuzikhumbitso za mphoto osati chikondi. Alaliki ena amalonjeza kuti Mulungu awabwezera mphatso ndi madalaitso andalama. Posokoneza malemba posawatanthauzira molinga ndi cholinga cheni cheni cha malembawo, amalonjeza mphotho zowirikiza pamene apereka kwa Mulungu. Kupereka kumeneko sikupoereka kwa Kulambira kwa chikondi, koma kulingati kugula tikiti ya njuga imene operekayo amayembekezera ku pata mphoto ya pamwamba kwambiri! Palibe pamene mu Baibulo mu akunena zakupereka kotero.

Koma kuti, Bibulo lalemba zakupereka kwa Maliya. Pamene anazoza Yesu, panalibe mphoto yoneka pamaso. Anakhuthula chuma chake chomwe amkasungira osaganizira zomwe mwe amayenera kuti alandire. Ngakhale ophunizra anakwiya chifukwa cha kuwononga kumeneku. Ndi Yesu yekha anawona namutamnda chifukwa cha mphatso yake, mphatso imene inatakatsidwa chikondi chokha basi (Mateyu 26:6-13).

Kupereka kwa Kulambira sikungotakatsidwa kokha ndi chikondi cha Mulungu chokha, komanso ndi **chikondi cha apa anthu ena**. Yohane anawakumbutsa anthu ake owerenga kuti chikindi cheni cheni mchoposa mawu; ndi chatchito. Chikondi cha Afilipi pa Paulo chinaoneka kudzera mkuoereka. Chikondi cha okhulupirira chimaonekra pa kupereka.

> Komai ye amene alinacho chuma cha dziko lapansi nawona mbale wake ali wosowa, ndi kutsekereza chifundo chache pommana iye, naga chikondi cha Mulungu chikhala mwa iye bwanji? Tiana, tisakonde ndi mawu, kapena ndi lilime, komatu ndikuchita ndi choonadi (1 Yohane 3:17-18).

Kupereka kwa kulambira ndi kowolowa manja osati kowumira.

Paulo anatsikimizira mpingo wa ku Akorinto kupereka koolowa manja pamene anati, "Polemeretsedwa inu mzonse ku kuolowa manja konse kumene kuchita mwa ife mchiyamiko chakwa Mulungu. Pakuti utumiki wakutumikira kumene suudzaza mzosowa za oyera mtima koma uchulukirannso kwa Mulungu mamayamiko ambiri" (2 Akorinto 9:11-12). Kuti kupereka kukhale kolambira koona kukuyenera kukhale kopereka moolowa manja.

Kupereka kokhala ndi kulambira kumalimbikitsidwa ndi kudzichepetsa osati kunyada.

» Werengani Mateyu 6:1-4.

Muchiphunzitso cha pa Phiri, Yesu anachenjeza za malingaliro olakwikwa pakupereka. Ena amapereka kuti ayamikiredwe ndi ena; mphoto yawo ndi kuyamikiridwa. "alandiriratu mphoto yawo." Ena amapereka mwa kachetechete, akuzitamandira okha pakudzichipetsa kwawo; mphoto yawo ndi khutitsidwa kwaiwo eni. Yesu anati, "Musalole dzanja lamamzere lidziwe chomwe dzanja lanu lamanja lichita." Musadziyamikire nokha chifukwa chakuwolowa manja kwanu. Mmalo mwake mulole Atate wanu wakumwamba awone nakupatseni mphoto monga afuna.

Nkhani ya Kupereka Mokondwera

John Wesley anali atangomaliza kugula zithunzi za mchipinda mwake ndi pamene wantchito wake wa mkazi anabwera pa chitseko chake. Kunazizira kwambiri tsiku limenero ndipo anawona kuti wantchito wakeyo anavala zovala delesi lopepuka kwambiri. Anapisa mthumba mwake nampatsa iye ndalama kuti akagule juzi, ndipo anapeza kuti anatsala ndi ndalama zochepa kwambiri mnyumba mwakemo. Analira kwambiri, "Ndakongoletsa khoma langa ndi ndalama zomwe zikanamutetedza munthu osowa uyu ku mphepo yozizira!"

Wesley anayamba kugwiritsa ntchito ndalama zake ndi kumasungira kuti apereke kwa osauka. Mukalata yake, analemba kuti kwa chaka ndalama yomwe amalandira inali $30, ndipo zomwe amagwiritsa ntchito zinali $28 choncho amatsala ndi $2 yomwe amaipereka.

Chaka chinachi, ndalama yake yolandira inawonjezeka kawiri koma anapitirira kugwirtsa ntchito $28 ndimapereka $32. Chaka cha chitatu ndalama zolowa zinadumpha kufika pa $90; iye anapitirira kugwiritsa ntchito $28 ndi kupereka $62. Chaka chachitatu anapeza $120, anagwiritsa ntchito $28 ndipo anapereka $92 kwa osauka.

Wesley analalikira kuti Akhristu asamangopereka chakhumi choka, koma kuti apereke mowonjeza. Anakhala ndi moyo owonjezera zolowa, kupereka kwathu kuziwonjezeka. Anachita izi mu moyo wake onse. Ngakhale ndalama zake zinachuluka kwambiri anakhala moyo ophweka napereka zapamwamba zake. Kwa chaka chimodzi ndamala zake zolowa zinafika $1,400; anapereka zonse natsala ndi $30.[67] Anati sanasungeko koposa $100. Anapereka zonse $30,000 zomwe anapeza m'moyo wake wonse.[68]

Cholinga cha nkhani iyi silamulo la umphawi! Cholinga ndi kumvera kokondwera ndi kofuna kwa Mulungu. Mulungu sapereka kwa aliyense mofanana ngati John Wesley. Yeso silakuti "Kodi ndikupereka zochuluka ngati wina aliyense?" Yesero ndi lakuti, "Kodi ndi kupereka mwa Chimwemwe ndi momvera kwa Mulungu?" Mulungu amatiitana kulambira ndi kupereka kodzipereka nsembe.

Mchitidwe wa Kupereka

Chifukwa kupereka ndi mchitidwe wa kulambira, zopereka ziyenera kutengedwa munjira zimene zimathandizira ku mzimu wa kulambira. Ganizirani za mfundo izi.

Kutsindika mu chopereka kukhale kulambira, osati zosowa.

Mwina chifukwa chimene Akhristu ambiri amawonera chopereka ngati njira yolipirira zinthu za pa mpingo ndichakuti kutsindika mu chopereka chili pakulipirira mitengo ya zinthu! Izi zimafika powonjeza pamene mavuto a zachuma atitsogolera kuti tinene, "mpingo utsekedwa" kapena "sitingatumize mtumwi" ngati chopereka chowolowa manja sichiperekedwa. Nthawi zina abusa amapepesa chifukwa chofunsa chopereka; "nkanakonda tikanapanda kufunsa za ndalama zanu." M'malo mwake chopereka chiyenera chikhale chionetsero cha kupereka mokondwera.

Pakutenga chopereka, cholinga chizikhala kulambira. Chopereka chikhoza kunenedwa ndi malemba amene amakumbutsa wolambira za cholinga cha chopereka. Malemba monga opezeka pa 2 Akorinto 8:9, 2 Akorinto 9:7, Eksodo 25:2, Machitidwe 20:35. Komanso pa Yohane 3:16 amalozera ku chilimbikitso choona cha kupereka.

---

67 Kuti tifaninzire lero, ndi chimodzimodzi ndi kupeza 200,000 ndi kupereka $5,000. Mu nthawi ya moyo wake, Wesley amapeza ndi kupereka $3,000,000 mu ndalama za lero.

68 Nkhani iyi yatengedwa kuchokera kwa, "Four Lessons on Money from One of the World's Richest Preachers" Christian History 19 (Summer 1988): 24. Available at https://christianhistoryinstitute.org/uploaded/50cf76d05900d6.14390582.pdf July 22, 2020.

Chopereka chiyenera kukhala mbali imodzi ya mwambo wa kulambira pachokha.

Mu zikhalidwe zina ndichachizolowezi kulimbikitsa anthu kupereka chopereka kupatula pa mwambo wa mapemphero pawokha. Pamene izi zikhoza kulimbikitsidwa ndi khumbo lopewa kudzionetsera kapena kusunga nthawi mu mwambo wa kulambira, zimalekanitsa kupereka ndi kulambira. Kutenga chopereka ngati mbali imodzi ya mwambo wa kulambira kumathandiza wolambira kumvetsetsa za kupereka ngati mwambo wa kulambira.

Pakuti kulambira ndi chimvomerezo chathu kwa Mulungu, mukhoza kuganizira zotenga chopereka pambuyo pa uthenga kusiyana ndi uthenga usanalalikidwe. Izi zikunena kuti, “Tikupereka kwa Mulungu pakuyankhira ku Mawu ake.”

Makolo ayenera aphunzitse ana awo kupereka mu kulambira.

Monga ngati m’mene timaphunzitsira ana athu kuyimba, kupemphera, ndi kumvetsera kuwerenga kwa malemba ndi ulaliki, tiyenera kuphunzitsa ana athu kupereka mokondwera. Pamene ana athu akuphunzira kuti kupereka ndi mchitidwe wa chimwemwe wa kutamanda, iwonso adzakhala wolambira.

Nyimbo mu nthawi ya chopereka ziyenera zikhale za kulambira.

Ngati kupereka ndi kulambira, nyimbo pa nthawi ya kupereka zikhale za kulambira. Izi zikhoza kukhala za zida zoyimbira kapenanso za akapela; ikhoza kukhala ya munthu m’modzi kapena mpingo onse; ikhoza kukhala ya kayaziyazi koma za tanthauzo kapena zachikondwerero komanso za mphamvu; osatengera mayimbidwe, ziyenera zikhale mbali imodzi ya kulambira. Amene amachita za nyimbo pa nthawi ya chopereka ayenera apempherere chitsogozo cha uzimu monga ngati m’mene wotsogolera kulambira amapempherera chitsogozo cha uzimu. Mbali ina iliyonse ya kulambira isatengedwe mwachibwana.

Chopereka chitsogozane ndi pemphero la mdalitso.

Pakuti chopereka ndi mphatso yopita kwa Mulungu, chopereka chiyenera kutsatana ndi pemphero loyeretsa. Izi zimakumbutsa wolambira za cholina chopereka ndipo zimapereka umboni owonekera wa kupereka ngati kulambira.

Atsogoleri a mpingo akhale oyang’anira abwino a mphatso za anthu.

Mu chopereka, wolambira akudalira mphatso zawo ku chisamaliro cha atsogoleri a mpingo. Atsogoleri a mpingo ayenera kukhala osamalira abwino a mphatso. Kusamalira gulu pa kagwiritsidwe ntchito ka ndalama kumaonetsa kuti zopereka zikugwiritsidwira ntchito ya Mulungu. Izi zimalimbikitsa kupereka komanso kuchepetsa ukamberembere mu utsogoleri wa mpingo. Mu dziko limene atsogoleri a Chikhristu amatengedwa osakhulupirika, tichite china chilichonse mwakuthekera kudzionetsa tokha opanda chilema.

Chopereka ndi choposera njira yoperekera mitengo ya zinthu; uwu ndi mchitidwe wa kulambira. Kudzera M'mawu ake, Mulungu amadzionetsera yekha kwa wolambira. Timamvomera ndi chopereka kuchokera m'mitima yathu yokondwera. Uku ndi kulambira koona.

FUFUZANI

Kodi anthu mu mpingo mwanu amamva ngati akulambira akamapereka, kapena akulipira mitengo ya zinthu? Kodi ndi ndondomeko zanji zodziwika zimene mungatenge kuti mupange kupereka kukhala mchitidwe wa kulambira?

MGONERO WA AMBUYE

» Kambiranani za mwambo wa mgonero wa mpingo wanu. Kodi mumakondwera motalikirana bwanji? Mukamachita mgonero, kodi imakhala mbali yofunikira kwambiri ya mwambo?

Monga ngati m'mene Mulungu amaonetsedwera mu **M'mawu** wolembedwa (Kuwerenga kwa malemba komanso **M'mawu** oyankhulidwa (kulalikira kwa Mawu ake), akuwonekera mu **mawu** onenedwa pa Mgonero Wa Ambuye.[69] Mgonero Wa Ambuye ndi chikumbutso cha imfa yowombola ya Yesu komanso chikondwerero cha kuukanso kwake. Mgonero omaliza unali ogwirizana ndi Paska, komanso unakhazikitsa za pangano latsopano.

» Werengani Mateyu 26:17-30 ndi 1 Akorinto 11:17-34.

"Mgonero ndi chikonzero cha kukumana kwa Ambuye ndi anthu ake. Iwo amene amasunga za chikonzekero cha kukumana uku akhoza kuyembekezera molimba mtima kuti adzabweradi kudzakumana nawo."

Franklin Segler ndi Randall Bradley

69 Franklin M. Segler and Randall Bradley, *hristian Worship: Its Theology and Practice* (Nashville: B&H Publishing, 2006), 178.

Malo olozera za Mgonero mu Chipangano Chatsopano ndi mu mabuku a Uthenga Wabwino ndi malangizo a Paulo ku mpingo wa kwa Akorinto.

Mafunso atatu nthawi zambiri amafunsidwa potengedwe ka Mgonero Wa Ambuye.

- Kodi tanthauzo la Mgonero wa Ambuye ndi chiyani?
- Kodi Mgonero wa Ambuye uyenera kuchitika motalikirana bwanji?
- Kodi Mgonero wa Ambuye uyenera kuchitika motani?

Kodi Tanthauzo la Mgonero wa Ambuye ndi Chiyani?

Kuchita Mgonero ndi mbali ya tanthauzo lalikulu la kulambira.[70] Pakulembera mpingo wa kwa Akorinto, Paulo anawonetsa kuti mu Mgonero wa Ambuye:

1. Tikuyang'ana ku imfa ya Yesu ("mumalengeza imfa ya Ambuye").
2. Tikudikira kubweranso kwa Khristu ("Kufikira atabweranso").

Pamene tikondwerera Mgonero, timakumbukira nsembe yake, ndipo timayembekezera lonjezo lake la kubweranso. Zipangizo zimayimira thupi ndi mwazi wa Khristu ndipo zimatikumbutsa za kutengapo mbali kwathu pa imfa ya Ambuye. "Pamene tidalitsa chikho cha Mgonero wa Ambuye, mothokoza Mulungu, kodi sitikugawana magazi a Khristu? Nanga buledi amene timanyemayo, kodi sitikugawana thupi la Khristu?" (1 Akorinto 10:16). Mgonero wa Ambuye ndi chizindikiro cha mphamvu cha kupezeka kosatha kwa Ambuye wopachikidwa ndi owukitsidwa.

Kodi Mgonero wa Ambuye Uyenera Kuchitika Motalikirana Bwanji?

Malemba ngakhalenso mbiri ya mpingo siipereka yankho lofotokozera funso ili. Mu mpingo woyambirira zikuwonetsa kuti Mgonero wa Ambuye umachitika tsiku la Sabata iliyonse. Lero, mipingo ina imakondwerera Mgonero sabata ndi sabata pamene ena amachita kamodzi kapena kawiri pachaka.

Ngati Mgonero wa Ambuye ndi ganizo logwirizana ndi woyenera pa kulambira, kuchita mwambo kawirikawiri sikuchepetsa tanthauzo la Mgonero kusiyana ndi kuwerenga kwa Baibulo kwa sabata iliyonse kumawononga kufunikira kwa malemba mu kulambira.

---

70 Chithunzi: "Mgonero wa Ambuye" taken by Allison Estabrook on Oct. 14, 2022, retrieved from https://www.flickr.com/photos/sgc-library/52476662295/, licensed under CC BY 4.0.

Kodi Mgonero wa Ambuye Uyenera Kuchitika Motani?

Paulo anachenjeza Akorinto za kudya ndi kumwa "mosayenera" (1 Akorinto 11:27).[71] Njira zina zikhoza kutithandiza pa kutenga Mgonero wa Ambuye mu njira yoyenera kwa Akhristu.

Mgonero uyenera ukhale gawo lalikulu la mwambo wa kulambira, osati mwambo owonjezera chabe.

Nthawi yabwino ya Mgonero wa Ambuye ndi yotsatana ndi uthenga. Pa ichi, uthenga uyenera utitsogolere pa kumvetsa kozama kwa Mgonero. Izi zikhoza kuchitika kudzera mu uthenga olalikidwa mwa chindunji wa Mgonero wa Ambuye, kapena uthenga wa mutu ogwirizana nawo (chiwombolo, kuwombola, chisomo, kupanga ophunzira). Kwa mipingo imene imakondwera Mgonero wa Ambuye pafupippafupi, sikoyenera kukhazikitsa cholinga cha mwambo wa mapemphero pa Mgonero ndi mwambo optilira.

Mgonero ndi mwambo wa ulemu komanso osangalatsa.

Nthawi ya Mgonero ndi nthawi yakudziyesa wekha motsimikiza mtima komanso mwa chikondwerero cha chisomo cha Mulungu. Kutsimikizika mtimaku kumaonekera mu chikumbutso chakuti Mgonero umadyedwa pokumbukira imfa ya Ambuye. Chikondwerero cha kusamalira chimenechi chimaonekera mu lonjezo la kubweranso kwa Ambuye.

Pa mwambowu, chikondwerero cha kuukanso ndi chiyembekezo cha kubweranso kwa Khristu zikhoza kukhala cholinga choyambirira cha Mgonero. Nthawi zina, ulemu wa imfa ya Yesu ndi kufunikira kwa kudziyesa zikhoza kukhala cholinga choyambirira. Mbali zonse ziwiri ndi gawo ya kukumbukira.

Timakondwera mu Mgonero chifukwa Mgonero wa Ambuye umatheka chifukwa cha chisomo cha Mulungu. Pa Mgonero wa Ambuye, timakumbutsidwa kuti chisomo chokha chimapereka chipulumutso chathu. Timavomereza ulemu wa Mgonero chifukwa timakumbukira kuti kutengapo mbali kwathu pa Mgonero wa Ambuye kumayimira kudzipereka kukusiya chimo. Pa Gome la Ambuye, wolambira aliyense ayenera kudziyesa.

Mgonero uyenera kuwonetsera umodzi wa mpingo.

Ndi zachisoni kuti Mgonero umene cholinga chake chinali kuwonetsera umodzi wa mpingo, nthawi zina wakhala choyambitsa mgawano. Kusiyana kwa m'mene Mgonero wa Ambuye uyenera kukhalira (chikho chakechake, chikho cha onse, kususa mkate m'chikho) komanso

---

71 Kumasulira kwa KJV kwa "amwa mosayenera" nthawi zina anatanthuzidwa kunena kwa munthu amene siwoyenera, ku Mgonero wa Ambuye. Koma, "mosayenera" akuwoneka kukhala kumasulira kwabwino. Palibe amene ali woyenera nsembe ya Yesu. Vuto lofunika kukonzedwa pakati pa anthu a ku Korinto sikunali kusayenera kwa wolambira, koma kusalemekeza, kusayenera kumene iwo amachitira chakudya chopatulika.

kusiyana kwa ndani amene angalandire nawo (Akhristu onse omvomerezeka, okhawo amene anabatizika, mamembala okhawo a mpingo wa pamalo) zayambitsa mikangano pakati pa mipingo.

Paulo anakumbutsa mpingo wa kwa Akorinto kuti pamene agawana mkate umoodzi, akhale thupi limodzi. “Pakuti buledi ndi mmodzi yekha, ifenso ngakhale tili ambiri, ndife thupi limodzi, popeza tonse timagawana buledi mmodzi yemweyo” (1 Akorinto 10:17).

Tiyenera kukumbukira kuti mu Mgonero wa Ambuye, kulambira ndiye kofunikira kuposa zonse ndipo ndondomeko zikhala zotsatirapo. Mpingo uyenera kusunga ndi kupititsa patsogolo ndondomeko zokhulupiririka pakati pa mauthenga abwino ndi mu 1 Akorinto. Mwina mulimonse m’mene Mgonero umakonzedwera, pasakhale zogawanitsa anthu. Mu Mgonero wa Ambuye, timakondwerera chiyanjano cha banja la Mulungu.

KUMALIZA: MPHAMVU YAYIKULU YA KULAMBIRA

Kodi Kulambira ndi kofunkira? Apa pali umboni wa 1945 umene ukuonetsa zimene zingachitike pamene munthu wamba alambira kudzera mu pemphero.

Mu nthawi ya Nkhondo ya Dziko Lonse, munthu wotembenuka mtima wa chipembedzo cha Chibuda wophunzira ku America-wochokera ku Japan pa sukulu ya ukachenjede ya Baylor anakhala chida cha chitsitsimutso. Reiji Hoshizaki anagwira ntchito ngat woyang’anira pamalo kuti alipire sukulu. Pamene anali kukoza m’makalasi, anayamba kupempherera desiki lililonse.

Tsiku, lina patatha masabata a pemphero, Reiji anakhala pansi atatopa ndi zolemetsa za anzake a mkalasi anagwada pa mawondo ndi kuyamba kulira ndi kupemphera. Ophunzira anafunsa, “Kodi chavuta ndi chiyani, Reiji?” Palibe chimene chinalakwika ndi Reiji; mpando wake unasanduka guwa.

Kudzera mu kupembedzera kwa Reiji, chitsitsimutso chinafalikira pa sukulu ya ukachenjede ya Baylor kenaka ku dziko la Texas. Makumimakumi a ophunzira olalikira anachoka pa sukulu ya ukachenjede ya Baylor kupititsa chitsitsimutso kummwera cha kumadzulo kwa United States. Pemphero ndi gawo lofunikira la kulambira. Pamene tikulambira, dziko lathu limasinthika ndi mphamvu ya Mulungu.

KUBWEREZA KUONANSO PHUNZIRO 7

1. Tikhoza kupanga uthenga kukhala thima mu kulambira pakuyika malemba mu madera onse a kulambira.

2. Pakuti malemba ndi ofunikira pa kulambira, tiyenera kuwonetsetsa kuti akuwerengedwa bwino, mwamphamvu, ndi mawerengedwe amene adzapangitsa kuwerenga kukhala kokhazikika.

3. Pakuti kulalikira ndi mbali imodzi ya kulambira:

   - Kulalikira kumafunika kukonzekera mosamala.
   - Kulalikira kumafunika kuvomereza kuchokera kwa anthu onse.
   - Kulalikira kumafunika kuvomereza kochokera kwa mlaliki.
   - Mlaliki ayenera kupatsidwa mphamvu ndi Mzimu Woyera.

4. Njira zodziwika zopanga pemphero kukhala gawo la tanthauzo la kulambira kwa gulu:

   - Khazikitsani moyo wanu wa pemphero la mseri.
   - Phunzirani kupemphera.
   - Pempherani mawu a malemba.
   - Khazikikani pa kuyanjana ndi Mulungu.
   - Lumikizitsani zofuna zanu ndi za Mulungu.
   - Yankhulani ndi Mulungu, osati mpingo.

5. Pakuti kupereka ndi mbali imodzi ya kulambira:

   - Kupereka kulimbikitsidwe ndi chisomo, osati mantha.
   - Kupereka kulimbikitsidwe ndi chikondi, osati mphoto.
   - Kupereka kukhale kowolowa manja, osati kowumira.
   - Kupereka kulimbikitsidwe ndi kudzichepetsa, osati kudzikweza.
   - M’mene timatengera chopereka ziyeneranso kuchitapo kanthu pa mzimu wa kulambira.

6. Mgonero wa Ambuye

   - Umayang’ana ku imfa ya Khristu.
   - Umayang’ana pa Kubweranso kwa Khristu.
   - Uyenera kutengedwa moyenera.
   - Uyenera kutengedwa mwa ulemu ndi mokondwera.
   - Uyenera kutengedwa mwa njira imene ima.

NTCHITO YA PHUNZIRO 7

1. Mu phunziro 6, munasankha nyimbo zogwirizana ndi mitu isanu yosiyana. Mwa lililonse la mitu isanu imeneyi, pezani ndine zitatu kapena zinayi zimene zikuyankhula ku phunziro. Mndandanda wanu udzagwiritsidwa ntchito mu phunziro lotsatira pamene mukukonzekera mwambo wa kulambira.

    - Mavesi atatu kapena anayi pa chikhalidwe cha Mulungu
    - Mavesi atatu kapena anayi pa imfa ya Yesu ndi kuuka kwake
    - Mavesi atatu kapena anayi pa Mzimu Woyera ndi mpingo
    - Mavesi atatu kapena anayi amene amayitana anthu a Mulungu ku moyo wogonjera, wa chiyero
    - Mavesi atatu kapena anayi pa chisokole ndi utumwi

2. Kumayambriro kwa phunziro losatira, mudzalemba mayeso ochokera pa phunziro ili. Werengani mafunso a mayeso mosamala pa kukonzekera.

MAYESO A PHUNZIRO 7

1. Tchulani zitsanzo zitatu zowonetsa kufunikira kwa malemba mu kulambira.
2. Tchulani mbali zitatu za mwambo wa kulambira pamene malemba akhoza kugwiritsidwa ntchito.
3. Tchulani zotsatira zinayi zodziwika za mfundo yakuti *Kulalikira ndi Kulambira*.
4. Perekani maganizo atatu odziwika a kupanga pemphero kukhala gawo la tanthauzo la kulambira kwa gulu.
5. Tchulani mfundo zinayi za kulambira kwa tanthauzo.
6. Tchulani mfundo zinayi zodziwika zopangitsa kupereka kukhala m'chitidwe wa kulambira.
7. Tchulani mfundo zitatu za mgonero zovomerezeka mu 1 Akorinto.
8. Lembani Mateyu 6:5-8 kuchokera pakuloweza.

PHUNZIRO 8

KUKONZEKERA NDI KUTSOGOLERA KULAMBIRA

ZOLINGA ZA PHUNZIRO

1. Kuzindikira kufunika kwa kukonzekera mwa uzimu pa kutsogolera kulambira.
2. Kuzindikira ntchito ya dongosolo komanso mutu wa cholinga pa mwambo wakulambira.
3. Kukonzekera mwambo wolinganizidwa bwino wa kulambira umene umafikira thupi lonse la Khristu.
4. Kuzindikira zoyenereza zimene zimafunikira mtsogoleri wa kulambira.
5. Kusiyanitsa pakati pa utsogoleri ndi kutsogolera mwambo wakulambira.
6. Kuchita njira zoyenera za utsogoleri wa kulambira.

KUKONZEKERA PHUNZIRO ILI

Lowezani 2 Mbiri 5:13-14.

CHIYAMBI

» Kodi ndi nthawi yokonzekera yochuluka bwanji imene mumaipereka ku kulambira kwa sabata iliyonse? Kodi mumafananitsa nyimbo ndi uthenga? Kodi kukonzekera kotere ndikoyenera? Kapena kukonzekeratu kumasokoneza machitachita a Mzimu Woyera munthawi ya kulambira?

Ganizirani za mayi amene akukonzekera chakudya cha Alendo olemekezeka. Pamene alendowo akufika kuti adzadye, mwini khomo amvekere, “ine sindimakhulupirira zotenga nthawi yochuluka pokonzekera chakudya. Tengani mkate uwu wotsalira, nyama, komanso ndiwo za masamba. Ingoziphatikizani umo mungafunire.” Kodi mungachitire izi alendo olemekezeka? Ayi ndithu! Mumafuna kupereka zabwino kwa alendo anu.

Taganizirani abusa amene akubwera ndi kulambira kwa Mulungu ngati mphatso. Amvekere, “Ine sindikhulupirira kutenga nthawi yochuluka kukonzekera kulambira. Ndimafuna kumupatsa mpata Mzimu Woyera kuti ayankhule kudzera mwa ine, choncho sindikonzekera kalikonse. Koma ndimangomulola Mzimu anditsogolere.”

Atsogoleri ena amakhulupirira kuti Mzimu Woyera sangagwire ntchito mu uthenga komanso mwambo wolambira umene wakonzekeredwa bwino. Koma Baibulo limationetsa kufunika kokonzekera mwambo wa kulambira. Kuyambira kuwakonzekeletsa moyenera oyimba kumwambo wolambira wa Kachisi, mpaka kufikira ku chitsogozo cha Paulo pa nkhani ya mwambo wakulambira mu mpingo wa ku Akorinto, Malemba amawonetsera kuti kukonzekera ndikofunika pa utsogoleri mu utumiki. Tisamabweretse chopereka chopanda mtengo. Chifukwa chakuti kulambira ndiko kudzipereka mtengo kwathu kwa Mulungu, Mulungu amafunika chopereka chabwino.

Mu phunziroli tiona mfundo ziwiri za utsogoleri wa kulambira. Choyamba, tiphunzira kufunika kwa kukonzekera mwambo wolambira. Kenako tiwona utsogoleri woyenera pa nthawi ya mwambo wolambira.

KUKONZEKERA MWAMBO WA KULAMBIRA

» Werengani Eksodo 28-29. Onetsetsani mosamala amene anali kutsogolera mwambo wa kulambira ku Israele. Kodi mumadzikonzekeretsa bwanji kuti mutsogolere mwambo wa kulambira kumbali ya uzimu, malingaliro komanso maimvaimva?

Kukonzekeretsa Otsogolera Kulambira

Dongosolo ndi kukonzekera mwambo wa kulambira ndikofunika kwambiri; Kukonzekeretsa **Otsogolera kulambira** ndikofunikanso kwambiri. Sitingatsogolere anthu kumene ife sitinafikeko. Pachifukwa ichi tikuyenera kukonzekeretsa mitima yathu tisanayesere kutsogolera ena mu kulambira.

Mu Phunziro 2, tinawona zoyenereza za Mulungu kwa wolambira. Mulungu amafuna womulambira azikhala ndi manja woyera komanso mitima yoongoka. Tisanayambe kukonzekera mwambo wa kulambira tikuyenera kudzikonzekeretsa tokha ngati atsogoleri. Tikuyenera kukhala okonzeka muuzimu kutsogolera kulambira.

Yambani kukonzekera mwambo wakulambira ndi pemphero komanso kuwerenga malemba. Tengani nthawi kuwerenga Mawu a Mulungu kuti mukuze moyo wanu wa uzimu. Choopsa kwambiri kwa otsogolera kulambira ndiko kutsogoza kukonzekera utumiki ndikusiya kukuza uzimu. Timatha kuwerenga Baibulo pokonzekera uthenga wa ena pamene tikulephera kulola Mawu Mulungu kuti ayankhule ku zosowa zathu za uzimu.

Musanasankhe malemba komanso nyimbo zimene zimayankhula Mawu a Mulungu ku mpingo onse, tengani nthawi kulola Mawu Mulungu komanso Mzimu wa Mulungu kuti ayankhule kwa inu panokha monga munthu. Ndipo pamene mukuyamba kukonzekera mwambo wa tsiiku la Sabata, mufunseni Mulungu akutsogorereni ku malemba, Mutu wa uthenga, ndi nyimbo zimene zidzayankhula ku zosowa za anthu.

"Munthu amene amatsogolera ena pamaso pa Mfumu ayenera kukhala woti anayenda m'dziko la Mfumu ndi kuona nkhope ya Mfumu nthawi zambiri."

Charles Spurgeon

FUFUZANI

Kodi mumakonza bwanji makhalidwe abwino a kulambira kwa panokha? Kodi mumakumana ndizolepheretsa zotani? Nanga mumathana nazo bwanji zolepheretsazo?

Kukonzekera Mwambo wa Kulambira[72]

Fred Bock anafotozera kukonzekera kwa m'busa amene anali kutumikira pansi pake, Lloyd John Ogilvie. Dr Ogilvie anakonzekera ulaliki wake kwa chaka chonse. Nthawi zambiri uthenga woti wakonzedwa mu mwezi wa January umadzakhala ndi tanthawuzo kuzosowa za athu ukalalikidwa mu mwezi wa July. Chifukwa chiyani? "Mulungu wathu ndi Mulungu

72 Zambiri zokhudza kukonzekera kulambira zimapezeka mubuku lotchedwa "The Nuts and Bolts of Worship" limene limapezeka pa tsamba la http://worship.calvin.edu/resources/resource-library/the-nuts-and-bolts-of-worship-planning zinaonedwa pa July 22, 2020.

wa dzulo, lero, komanso Mawa. Iye amadziwiratu zosowa zathu za mtsogolo, isanafike nthawiyo... ndipo panthawi imene takonzekera komanso tayika ndondomeko bwino bwino, zimatipangitsa kuti tikhale ofunikira, chida chofunika pamaso pa Mzimu Woyera."[73] Mzimu Woyera amadziwa bwino lomwe amene akapezeke ku mwambo wamapemphero; ndipo atha kukutsogolerani ku nyimbo komaso mau a Mulungu amene adzayankhula kolingana ndi vuto lawo.

Mwina musamakonzekere chaka chonse nthawi ina, koma kukonzekera mwambo wolambira ndikofunika. Kukonzeka mosamala bwino kumathandiza kuti nthawi yolambira ikafika umayika chindunji polambira osati kumakhalanso ndi nkhawa. "Kenako chimachitika ndi chiyani?" Tikapanda kukonzekera, timapezeka kuti tikubweleza zimene tinachita sabata yapitayo. Kukonzekera kumatipanga kukhala aluso.

"Kudzidzimutsa kopanda dongosolo kukhoza kukhala chisokonezo, ndipo dongosolo lopanda kudzidzimuka likhoza kukhala lopanda moyo."

Franklin Segler ndi Randall Bradley

Yambani ndi kuyika dongosolo.

Ambiri mwa ife timakonda dongosolo mmoyo. Timakonda kuti tizidya kadzutsa mmawa ndipo mgonero madzulo. Timakonda kuwerenga buku kuyambira tsamba loyamba mpaka lomaliza osati kumangowerengapo osatsata ndondomeko ya masamba. Palibe waulendo amene angakonde kukwera ndege yopita kunja kenako ndikumva oyendetsa akuti, "sitinapange chitsankho cha njira yoti tidutse lero. Mmalo mwake tingonyamuka ndipo tiziona zochita mkati mwa ulendo." Timakonda dongosolo.

Dongosolo pa nthawi yolambira Mulungu simatisokoneza ufulu otsatira zimene Mzimu Woyera angafune titsate ngakhale zitasiyana ndi zimene tinakonza! Dongosolo limatitsogolera pa nthawi yolambira, pamene tikuperekanso mpata ku chitsogozo cha Mzimu Woyera ngati akufuna tichite moposera zimene tinakonzekera. Pa nthawi imene anali kukhazikitsa Kachisi, panali dongosolo lokonzedweratu, komabe kupezeka kwa Mulungu kudapangitsa kusintha dongosoo la mwambowu (2 Mbiri 5:13-14).

Mu Mlozera A muli mndandanda wa mmene atsogoleri ena amakonzekerera mwambo wakulambira. Mwina mukhoza kuzipeza kukhala zothandiza kutengera imodzi mwa njirazi pa mapemphero anu. Njirazi sizokakamiza koma zikhoza kupereka ndondomeko zimene zingakuthandizeni kutengera ku zosowa zanu.

73 Lois and Fred Bock, *Creating Four-Part Harmony*, (Carol Stream: Hope Publishing, 1989), 43.

Ndondomeko zina zokonzekelera mwambo wolambira ndi:[74]

1. **Ndondomeko zokhazikika pa ulaliki**

    - Kulalikira uthenga wa choonadi: kuyimba nyimbo za m'buku, kuwerenga malemba, ulaliki
    - Anthu achitapo kanthu kumvomereza choonadi: kuyitanira, chopereka, nyimbo yotsekera mwambo

2. **Ndondomeko kutengera ndi zochitika za anthu a Mulungu pa nthawi yolambira**

    - Anthu a Mulungu asonkhana: Kuyitanira mwambo wa kulambira nyimbo za matamando, pemphero
    - Anthu a Mulungu amamvera uthenga: kuwerenga malamba komanso ulaliki
    - Anthu a Mulungu achitapo kanthu Kutsatira ulaliki: Nyimbo zam'buku zoyitanira anthu, chopereka
    - Anthu a Mulungu atulutsidwa: Nyimbo yam'buku yotsilizira mwambo, Mawu amdalitso

3. **Ndondomeko yowonetsa kukambirana pakati pa Mulungu ndi anthu ake (Kutengera pa Yesaya 6)**

    - Mulungu amadziwonetsera yekha (ndime 1): kuyitanira ku kulambira
    - Anthu a Mulungu kuchitapo kanthu kudzera mmatamando komanso kuvomeleza (Ndime 3-5): Nyimbo ya M'buku ndi pemphero
    - Mulungu amalankhula ndi anthu ake (ndime 6-8): malembo komanso ulaliki
    - Anthu a Mulungu kuchitapo kanthu kudzera kudzipereka kwawo (ndime 8): nyimbo ya m'buku komanso chopereka
    - Mulungu atuma anthu ake (Ndime 9): Mawu a mdalitso

4. **Ndondomeko kutengera Buku la Masalimo 95**

    - Kulowa ndi chimwemwe cha chiyamiko (Ndime 1-5): kuyitanira pa kulambira, Nyimbo za m'buku zamatamando
    - Pitilizani ndi kulambira mwa ulemu (Ndime 6-7): Nyimbo za kudzipatulira kwa Iye, pemphero
    - Imvani mau a Mulungu (Ndime 7-11): Malembo ndi ulaliki

---

74 Ndondomeko zimene zaikidwa apa ndi zamwambo wa mapemphero onse. Atsogoleri ena a kulambira amagwiritsa ntchito kwambiri ndondomeko ku mbali ya nyimbo zokha mu msonkano wamapemphero. Sindinaphatikize zimenezi chifukwa zimasiyanitsa mwambo wolambira ndi msonkhano wa mapemphero onse. Mu Baibulo, kulambira kumaphatikiza msonkhano onse, osati nyimbo zapadera zopatulidwa ku uthenga.

Falitsani uthenga ofanana.

Malambiro amalankhula ndi Mulungu, komanso amalankhula ndi mpingo. Polambira, timabweretsa Mawu a Mulungu kwa wolambira. Pamene tikukonzekera msonkhano wa mapemphero, ndizothandiza kufunsa, "ndi uthenga wanji umene Mulungu akufuna kupereka kwa anthu ake mu msonkhanowu?"

Munasonkhanko mu msonkhano okhala ngati otelewu?

Nyimbo	• Bwenzi lathu ndiye Yesu (Phindu lopemphera) • Fuwulilani kwa Ambuye (Kuyitanira Kukulambira) • Tonse tikadzapita Kumwamba (Chiyembekezo chathu cha kumwamba)
Nyimbo za Padera	Idzani, Mzimu Woyera (Kuyitanira Mzimu Woyera ku miyoyo yathu)
Uthenga	Kuyitanidwa kwa Yona kuti apite ku Ninive – cholimbikitsa ku utumiki wa usodzi
Nyimbo yotsekera msonkhano	Idzani, ino ndi nthawi yolambira (Kuyitanira ku kulambira)

Ndi uthenga wanji umene ungatsale ndi anthu olambira? Sindikudziwa. Mu mphindi makumi asanu ndi anayi (90), timayimba zokhudza chitonthozo mu nthawi ya Mavuto, kumwamba, Mzimu woyera komanso zoyitanira ku kulambira – zonsezi kuzungulira ulaliki wokhudza utumiki wa usodzi. Kodi msabata yotsatirayo anthu adzakumbukira zokhudza kufalitsa uthenga? Kapena mwina; koma nkhani ndi yoti msonkhano sunalimbikitse zokhudza mutu wa ulaliki.

Tsopano taganizirani msonkhano wokonzedwa ndi mutu woti "Kuyitanidwa kwa Yona kuti apite ku Ninive":

Nyimbo	• Idzani, ino ndi nthawi yolambira (Kuyitanira ku kulambira) • O' kuti Malilime chikwi ayimbe (kulumikizitsa matamando athu ndi kufalitsa uthenga) • Yesu amapulumutsa (Kumangilira uthenga wathu wa utumiki okamba zofalitsa uthenga) • Anthu akufuna Ambuye (Imaonetsa kufunika kwa usodzi)
Uthenga	Kuyitanidwa kwa Yona kuti apite ku Ninive – cholimbikitsa ku utumiki wa usodzi

Nyimbo za Padera	Kotero ndikutumani (Kutumidwa kufalitsa uthenga)
Nyimbo yotsekera msonkhano	Ndidzamuka kulikonse kumene mufuna ndipite (Kumvomera kutumidwa kutumidwa)

Chifukwa chakuti atsogoleri akonzekera kuti msonkhano ufalitse uthenga pa mutu umodzi, ndichodziwikiratu kuti anthu akhala akumva uthenga wa Mulungu msabata yonse, kuwakumbutsa za kuyitanidwa kukafalitsa uthenga. Pamene akhale akudutsana ndi anthu amene alibe Yesu mkati mwawo, mwina adzakumbuka kuti "anthu akufunika Ambuye." Pamene akugwira ntchito lachiwiri, mwina adzakondwa kuti pokumbuka kuti "Yesu amapulumutsa" nakumumbuka kuti, pakuti Yesu anatipulumutsa ife, tikuyenera kugawana ndi ena chimwemwechi.

Kodi Mulungu akhoza kugwira ntchito ndi msonkhano popanda Mutu weniweni? Tikakonzekera mokwanira ndi mosamala bwino, timathandizira kuti anthu ayike chindunji pa uthenga. Kodi izi ndizofunikira nthawi zonse? Ayi. Chifukwa nthawi zina Mulungu amatha kugwiritsa ntchito mitu ingapo pa msonkhano umodzi ndi cholinga chofuna kufikira anthu mu mpingo mzosowa zawo zosiyana siyana. Chifukwa Mulungu sagwiritsa ntchito njira imodzi yokhayo. Komabe, Pakakhala mutu umodzi otsatira, zimathandiza kuti olambira akhale ndi chindunji cha uthenga umene ukulalikidwa mu msonkhano.

Pitirizani kulinganiza mu kulambira.

Tonse tili ndi zimene timakonda: Tili ndi chakudya chokondedwa, nyimbo yokondedwa, mabuku okondedwa, masewera okondedwa, komanso mabuku a mu Baibulo okondedwa. Panthawi yokonzekera msonkhano wakulambira, ndizofunika kuti mtsogoleri aziyikapo mitu ya ulaliki, uthenga, ndi nyimbo zosiyana siyana kupatula zimene iye amazikonda zokha. Mwambo wolambira woyanjanitsa mbali zonse umatumikira uthenga wabwino kumpingo wonse.

1. **Mwambo wolambira woyanjanitsa mbali zonse umawonetsera Mphamvu ya Mulungu komanso kupezeka kwa Mulungu pakati pathu.**

Mulungu ndi wammwamba amene amalamulira pa dziko lonse; Mulungu ndi Mulungu wopezeka amene amakhala pakati pa anthu ake. Timaona kuyanjanitsa mbali zonse mu Baibulo monse.

"Atawoloka Nyanja yofira, ana a Israele anayimba za mphamvu ya Mulungu; Ndithu Yehova, pakati pa milungu, ndani afanana nanu? Inu amene muli woyera, ndiponso wotamandika wolemekezeka, chifukwa cha ntchito zanu, zazikulu ndi zodabwitsa? Munatambasula dzanja lanu lamanja ndipo dziko linawameza. Ndi chikondi chanu chosasinthika mudzatsogolera

anthu amene munawawombola. Ndi mphamvu zanu munawatsogolera ku malo anu woyera" (Eksodo 15:11-13).

Yesaya anawona atakhala pa mpando wachifumu, atakwezedwa pamwamba. Anali wamkulukulu ndiwoyera pamwamba pa dziko lonse. Ambuye anakwezedwa, koma anayankhula ndi Yesaya namulamula kuti "Muka ndipo ulankhule ndi anthu..." (Yesaya 6:1-13).

Wolemba Masalimo anatamanda Mulungu; "Inu Yehova Ambuye athu, dzina lanu ndi la lamphamvudi pa dziko lonse lapansi! Inu mwakhazikitsa ulemerero wanu m'mayiko onse akumwamba. Kuchokera m'kamwa mwa ana ndi makanda, Inu mwakhazikitsa mphamvu chifukwa cha adani anu, kukhazikitsa bata adani ndi anthu obwezera zoyipa. Pamene ndilingalira za mayiko anu akumwamba, ntchito ya zala zanu, mwezi ndi nyenyezi, zimene mwaziyika pa malo ake, munthu ndani kuti Inu mumamukumbukira, ndi mwana wa munthu kuti inu mumacheza naye? Inu munamupanga kukhala wocheperapo kusiyana ndi zolengedwa zakumwamba ndipo mwamuveka ulemerero ndi ulemu. Inu munamuyika wolamulira ntchito ya manja anu; munayika zinthu zonse pansi pa mapazi ake; nkhosa, mbuzi ndi ng'ombe pamodzi ndi nyama zakuthengo, mbalame zamlengalenga ndi nsomba zam'nyanja zonse zimene zimayenda pansi pa nyanja. Inu Yehova, Ambuye athu, dzina lanu ndi lamphamvudi pa dziko lonse lapansi!" (Masalimo 8).

Tikamalambira, timapereka chidwi chathu ku ukulu komanso kupezeka kwa Mulungu kwa ife. Pamene tikulambira Mulungu tikayiwala ukulu wake, kulambirako kumakhala kwa chisawawa ngati tikulambira munthu mzathu amene safunika ulemu ndi kumumvera. Pamene kulambira kwathu kwasoweka kupezeka kwa Mulungu, timakhala ngati tikupembedza Mulungu amene ali patali ndipo sakusamala za ife. Pamene tikukonzekera kulambira Mulungu, tikuyenera kuyika chidwi pa mmene ubale wa Mulungu ndi anthu ulili. Tikuyenera kuwakumbutsa olambira kuti timawopa Mulungu; Komanso tikuyenera kukumbuka kuti timakondwera mwa Mulungu.

KUCHITA

Kulambira Mulungu amene ali wammwamba komanso opezeka pakati pathu kumatanthawuza kuti tiyenera kuyimba nyimbo zimene zidzaonetsera ukulu wake ("O Lambirani Mfumu") ndi nyimbo zimene zimawonetsa ubale wake ndi munthu ("Immanueli, Mulungu nafe"). Mu pemphero tidzamutamanda kamba ka ntchito zake za mphamvu, komanso tidzaonetsera zosowa zathu za pamtima kwa Iye mwini.

2. Kulambira kolinganiza ndi kwa pagulu komanso kwa aliyense payekha.

Buku la Masalimo limakamba za matamando a pagulu komanso a pamunthu aliyense payekha. Masalimo ena amakamba za matamando "athu"; pamene ena amati matamando "anga". Kukachisi, wolambira a Chiheberi anali kulambira pamodzi; ndipo kunyumba'; anali kulambira aliyense payekha. Nthawi zambiri Yesu anali kupita ku sunagoge kukapemphera pa gulu; komanso anali kukapemphera payekha kukalumikizana ndi atate wake (Luka 4:16 ndi Marko 1:35). Kulambira kwa Baibulo kunali kwa pa gulu komanso kwa aliyense payekha. Pakulambira, tikuyenera kumapereka mpata kuti mpingo wonse uzilambira pamodzi monga thupi limodzi, komanso aliyense payekha azitha kudzipatulira pawokha kwa Mulungu wawo.

KUCHITA

Kulambira kwa gulu komanso kwa aliyense payekha kumakhudza mbali zonse za msonkhano wamapemphero. Tidzayimba nyimbo tonse pamodzi ("Mulungu Wathu ndi Wamkulu"); tidzayimbanso nyimbo zoti aliyense alambire payekha ("Ndinu Mfumu Yanga"). Tidzapemphera kwa "Atate wathu wa kumwamba"; tidzakhala ndi nthawi yopemphera pagulu kuti aliyense apemphere koma pamodzi.

Nthawi zonse mu mbiri ya pemphero, pemphero lapagulu limakhala lovuta. Munthawi ino ya lamya za mu manja, matabuleti, kutumiza mauthenga komanso kupezeka kwa intaneti paliponse, titha kukhala mu mwambo wamapemphero muthupi pamene mu mzimu sitili limodzi. Kudzipereka pa nkhani ya pemphero la pagulu kumafunika kudzipatula ku zosokoneza zili zonse ndikulambira ngati thupi.

3. Kulambira kolinganizika kumakhala ndi zodziwika kale komanso zatsopano.

Kulinganiza koteleku kumayenera kuti kuzichitika osati kungokhala zongonena poti tili pamaso pa Mulungu, koma zimenezi ndi zofunika ngati tikufuna kuti mpingo wonse utenge nawo gawo polambira. Tikamakonzekera mwambo wolambira, tikuyenera kulinganiza nyimbo zodziwika ndi zatsopano.

Nyimbo zatsopano zikachuluka zimapangitsa kuti anthu ambiri azingowonerera osati kutenga nawo mbali polambira; Sangayimbe nawo chifukwa choti nyimbozo sakuzidziwa. Nthawi ina C.S. Lewis anadandaula kuti abusa ambiri amayiwala kuti "Yesu anawuza Petro kuti 'dyetsa nkhosa zanga,' osati phunzitsa agalu wanga njira zatsopano." Kuchuluka kwa nyimbo za chilendo zimapangitsa chidwi cha kulambira kukhala chovuta.

Komanso kuchuluka kwa nyimbo zodziwika kumayambitsa chizolowezi chopanda phindu. Mwambo umene uli ndi chilichonse chodziwikiratu umapangitsa kuchotsa chidwi ndi kusatengapo mbali.

Kukonzekera kulambira kukhale ndi zodziwika ndi zosadziwika. Mwachitsanzo, "Kodi Chikondi cha Atate ndi Chozama Bwanji kwa Ife?" ndi nyimbo yatsopano ya chiwombolo. Nyimbo imathera pakuti, "mabala ake analipira ngongole yanga." Nyimbo yatsopano iyi yowonetsa mtengo wa mawomboledwe ikanatsatana ndi nyimbo yodziwika ya "Yesu Analipira Zonse," kutiitana ife kuti tione nsembe ya Yesu. Kulinganiza kwa nyimbo yodziwika ndi yatsopano kumalimbikitsa mpingo kululambira kwa machitachita.

KUCHITA

Kulambira kumene kumalinganiza zodziwika ndi zakale kudzaphatikiza nyimbo zakale ndi zatsopano. Kudzaphatikiza kuwerenga kwa malemba kodziwika ndi kuwerenga kosadziwika kwambiri. Musanawerenge ndime zodziwika monga Yohane 3:1-21 pamene Yesu akuphuzitsa za kubadwa kwatsopano, tikhoza kuwerenga kuwerenga ndime yosadziwika kwambiri monga Ezekieli 36:16-38 pamene Mulungu akolonjeza kusambitsa Israel ndi madzi ndikupsatsa mtima watsopano kwa anthu ake. Ndime ziwiri zimenezi ndi zofanana mu zolinga. Kuziwerengera pamodzi zidzazamitsa chid ziwitso cha mpingo cha chiphunzitso cha Yesu mu Yohane 3.

Ngati mukuphunzitsa nyimbo yatsopano, phatikizani nyimbo yatsopano ndi nyimbo zodziwika. Tikayamba kulambira ndi nyimbo yosadziwika, mwambo umayamba mokaikitsa. Ndi chanzeru kutsegulira ndi nyimbo yodziwika kenaka ndi kuphunzitsa nyimbo yatsopano.

Mpingo ku Taiwan unali ndi luso la kaphuzitsidwe ka nyimbo zatsopano. Ambiri mwa anthu awo anali okhulupirira atsopano ndipo samadziwa zambiri mwa nyimbo zimene zimayimbidwa. Mpingo uwu umakhala ndi kuphunzira mapemphero alionse asanachitike. Mphindi makumi awiri mapemphero asanayambe, anthu amayimba nyimbo zimene zikhale mbali imodzi ya mwambo wa mapemphero. Woyimba piano amayimba mingoli kuti aliyense aphunzire mamvekedwe. Chifukwa chakuti uku kunali kuphunzira, mtsogoleri amayima ndikubwereza mawu kufikira mpingo utaphunzira bwino. Pakufika 10:00, anthu amayimba nyimbo zatsopano mwamphamvu.

Konzekerani ngati gulu.

Mlaliki akupereka langizo ili; “Kukhala awiri n’kwabwino kuposa kukhala wekha, chifukwa ntchito ya anthu awiri ili ndi phindu” (Mlaliki 4:9). Kukonzekera kwa kulambira kuyenera kukhale ntchito ya gulu. Aliyense wotengapo mbali pa utsogoleri wa mwambo wa kulambira akhale ndi udindo pakukonzekera.

Ngati m’busa, otsogolera nyimbo, ndi atsogoleri ena a mpingo akumana pamodzi kufunafuna chifuniro cha Mulungu, mphamvu ya onse okumana zimaphatikizana pamodzi. Pakugwira ntchito ngati gulu, zilimbiko za membala aliyense zimawonjezera ku kulambira.

Kozekerani za nthawi yaitali.

Palibe mwambo wa mapemphero umene umakhala ndi uthenga onse wa Baibulo, koma pakupita kwa nthawi tiyenera kupereka uthenga wa uthenga wabwino kwa wolambira athu. Aliyense wa ife ali ndi mitu yake imene amaikonda; tizidziika tokha kulalikira ndi kuyimba mitu imene siili yokondedwa kwa ife.

Abusa ena ndi atsogoleri amagwiritsa ntchito kalendala imakhala ndi ndondomeko ya mitu ya ziphunzitso za mu Baibulo mu zaka zitatu.[75] Ena amakonzekera sabata ndi sabata koma amakhala osamala kudutsamo mu uthenga onsewo wa malemba kwa nthawi yaitali.

Ngakhale mulibe ndondomeko ya kalendala, koma kudziwa kwa nyengo zofunikira za Akhristu zidzakutsogolerani ku zinthu zofunikira za uthenga wabwino. Nyengo zofunikira kwa Akhristu ndi:

- **Adventi** (masiku a Sabata anayi ofikira ku Khristmas): Chidwi cha pa kubwera kwa Yesu koyamba ndi kwachiwiri wa Khristu.
- **Khristmas**: Kukumbikira za kubadwa kwa Khristu.
- **Lenti** (masabta asanu ndi imodzi isanafike nthawi wa kukumbukira za imfa ya Yesu): Kumbukira masautso ndi imfa ya Yesu, komanso zofunikira kwa iwo otsatira ndi kukhulupirira Yesu.
- **Isita**: Kukumbukira za kuuka ndi kukwera kumwamba kwa Khristu.
- **Pentekoste**: Kukumbukira za Mzimu Woyera ndi mpingo.

Kaya mumatsatira ndondomeko yatsopano kapena kutsatira ndondomeko ya sabata ndi sabata onetsetsani kuti mpingo wanu ukumva uthenga wonse ngati mbali imodzi ya kulambira.

---

75 Zikupezeka pa intaneti pa http://lectionary.library.vanderbilt.edu/calendar.php July 22, 2020.

Pangani ndondomeko mwa mtendere.

Kulambira sikolunjika kwa ife; kulambira ndi nsembe yathu yopita kwa Mulungu. Kukonzekera kwathu kwa kulambira ndi mbali imodzi ya chopereka chimenecho. Timakonzekera kulambira popanda kukakamizidwa koganiza kuti, "Kodi izi ndi zabwino?" Timabira Mulungu wa chisomo chopereka chathu chimalandiridwa chidukwa chakuti ndi chabwino, koma chifukwa chakuti Mulungu amalola chopereka chofun cha ana ake.

Izi ndizofunika pofuna kupewa nthangwanika zofuna "kufanana ndi mipingo monga yakutiyakuti" Munthawi ya lero lino ya luso la ma kompyuta komanso za kanema, mipingo yambiri ikumakhala pa mpanipani wofuna kukhala ngati mipingo ina. Abusa ali kalikiliki kupikisana kuti akhale ndi luso latsopano la compyuta. Otsogolera nyimbo ali alikiliki kuti ayimbe nyimbo zatsopano. Akhristu nawonso ali kalikiliki kusaka mpingo umene kuli zatsopano zimene zingathe kuwakopa.

Musagwe nkuyesedwa kofuna kusangalatsa Mulungu ndi zopereka zanu. Musalole kuti zida zogwiritsa ntchito polambira monga mayimbidwe kapena luso la makompyuta zisokoneze kulambira kweni kweni. Idzani kwa iye ndi monga mwa kukwanitsa kwanu ndipo Mulungu wodzala ndi chisomo adzakondwa nazo msembe zanu zonunkhira zochoka pansi pa mtima wanu. Mpatseni iye monga mwa kukwanitsa kwanu, ndipo khulupirirani kuti iye adzalandira zopereka zanu. Kulambira Mulungu si mpikisano woti mupikisane ndi mpingo wina; ndi mphatso imene timapereka kwa Mulungu.

KUTSOGOLERA MWAMBO WAKULAMBIRA

Funso lofunika kwambiri: *anthu amene mukuwatsogolera ndi ndani?*

» Kodi ntchito ya mpingo ndi chiyani pa nthawi yolambira? Kodi ntchito ya otsogolera matamando ndi yotani? Kodi ntchito ya Mulungu ndi yotani?

Anthu ambiri amatenga nthawi yolambira ngati mpikisano wa mayimbidwe. Mpingo umangomvetsera pamene abusa akulalika komanso pamene oyimba akuyimba. Ndipo Kachisi ndi nyumba yoyimbiramo.

Barry Liesch anatcha maonedwe otere a mwambo wolambira kukhala ngati masewera a mpira wa miyendo:[76]

- Wotsogolera matamando amakhala ngati ndi osewera ndipo akulambira.
- Mpingo wonse ndi anthu owonerera amene ali mu bwalo la masewero kuwonerera.

76 Barry Liesch, *The New Worship*, 2nd edition (Grand Rapids: Baker Books, 2001), 123.

- Mulungu ndiye mphunzitsi wa masewero amene amawuza atsogoleri a matamando chochita.

Chithuzithuzi cha mwambo wa kulambira kuchoka mu Baibulo ndichosiyanilanatu. Kutengera mu Baibulo, mpingo wonse umalambira pamene otsogolera amakhala ngati aphunzitsi amene amatsogolera kulambirako:

- Otsogolera matamando ndiye mphunzitsi otsogolera mpingo wonse.
- Olambira onse ndiwo osewera mpira amene amakhala akulambira.
- Mulungu ndiye owonerera amene amakhala akulandira matamando ndi malambiro athu.



Pa masewero a zisudzo, otsogolera samakhala powonekera. Otsogolera amadziwa sewero lonse mmene likuyendera ndipo amakumbutsa osewera aliyense ikafika nthawi yake yoti alowe m'bwalo. *Otsogolerayu akagwira ntchito yake bwino, owonerera samamuzindikira.* Imeneyo nde ntchito ya wotsogolera matamando. Ife ntchito yathu siyolambira kuti anthu azionerera; koma ntchito yathu ndiyotsogolera mpingo. Mpingo umalambira, pamodzi ndi abusa komanso otsogolera mayimbidwe, pamaso pa Mulungu. Cholinga chathu pa nthawi yolambira ndiko kukondweletsa Mulungu. Kolingana kalambilidwe ka mu baibulo, Mulungu ndiye owonerera malambiro.



Komabe, Mulungu amaposera anthu owonerera masewero; Mulungu amapereka mphamvu pa kalikonse kamene chimachita pa nthawi yolambira. Ndipo wotsogolera matamando ali oposera mphunzitsi wa masewero. Otsogolera matamando ndi mphunzitsi komanso wolambira. Kulambira kumaphatikizanso kupanga ubale:

- Mulungu amayitana wolambira, amalandira wolambira, ndipo amatsogolera atsogoleri a mwambo wolambira pamene ali kutumikira ku mpingo.
- Atsogoleri a mwambo wa Kulambira amatsogolera mpingo kulambira, amamvetsera Mawu a Mulungu, ndi kutenga mbali ngati wolambira.
- Mpingo umapereka malambiro kwa Mulungu amamvetsera Mawu a Mulungu, ndi kuyankhulana wina ndi mzake mwakulambira.



Mmene Mungapewere Kulambira ngati Msangulutso[77]

1. Yimbani nyimbo zakuti anthu amazidziwa aena zakuti akhoza kuphunzira mosavuta. Imbani mmawu osavuta a mpingo onse. Gwiritsani ntchito nyimbo zatsopano zosavuta.

2. Yimbani ndipo mukondwerere mphamvu, ulemerero ndi chipulumutso cha Mulungu. Tumikirani mpingo wanu. Adzazeni ndi Mawu a Mulungu. Osayamba nyimbo mamvekero oyipa kapena chikhulupiriro choooka.

3. Khalani ndi tcheru. Siyani kuyankhula kwambiri. Musalole kutalika kwa nyimbo/miwuni/zowonera kuti zikhale zotulutsira luso lanu mmalo mwa thima lla uthenga wabwino.

4. Tengerani kutsogolera kwanu kwa kulambira ndi nyimbo zimene mumasankha ku gulu la mpingo wanu. Tsogolerani mwa ubusa.

5. Lunjikani kwa Yesu. Osatenga chidwi kukhala pa inu.

Zoyenereza za Wotsogolera Kulambira

Pakusatengera udindo, ngati wotsogolera kulambira mumatumikira udindo wa ubusa. Ngati ndinu m'busa, mukudziwa kale izi. Ngati ndinu mkulu wa mpingo, muyenera kudziwa kuti udindo wanu umakuikani pa utsogoleri wa uzimu.

Pakusankha mtsogoleri wa kulambira, tiyenera kuganizira za zoyenereza za uzimu, osati zoyenereza za mayimbidwe kapena za umunthu. Pamene atumwi anasankha otumikira kuti asamalire amayi a asiye a Chihelene anayang'ana anthu a mbiri yabwino, komanso

77 Adapted from Jamie Brown, "Are We Headed For A Crash? Reflections on the Current State of Evangelical Worship." Available at https://worthilymagnify.com/2014/05/19/crash/ July 22, 2020.

khalidwe linali lofunikira (Machitidwe 6:3). Makhalidwe a kuthupi, uzimu komanso moyo anali ofunikira.

M'mipingo ina, chisankho cha otsogolera nyimbo, oyimba, komanso ma udindo ena a utsogoleri amachokera pa kutchuka. Otumikira amene anatumikira magome amasankhidwa chifukwa cha zoyenereza za uzimu, mwachidziwikire atsogoleri ayenera kusankhidwa chiukes cha zoyenereza za uzimu.

Ngati mumatsogolera kulambira mu mpingo mwanu (ngati m'busa, woyimba, kapena mtsogoleri wina mu kulambira), muyenera kufuna kukhala ndi makhalidwe amene amapanga mtsogoleri wa kulambira wamphamvu.

- **Chidziwitso cha uzimu**. "Kodi ndimakhala womvetsera kwa Mzimu Woyera?"
- **Nthumazi**. "Kodi ndine wa tcheru ku zosowa za mpingo? Kodi ndimasankha nyimbo ndi malemba zimene zimayankhula ku zosowa zimenezo?"
- **Mgwirizano**. "Kodi ndimatumikira bwino pagulu? Kodi ndimakhala omvetsetsa abusa akanena kuti ndisinthe nyimbo yotsekera? Kodi ndimasala ku zosowa za gulu lonse?"
- **Chidziwitso**. "Kodi ndikukula mu chidziwitso changa cha Mawu a Mulungu? Kodi ndimapanga Mawu a Mulungu kukhala thima mu kulambira?"
- **Nzeru**. "Kodi ndikukula mu nzeru kuti ndimvetsetse ndi kuchitapo kanthu pa kulimbana kwa kulambira? Kodi ndimadzipatsa mwambo kukhala womva msanga ndi kukhala wochedwa kuyankhula?" (Yakobo 1:19).
- **Kupirira**. "Kodi ndine opirira mpingo ukamachedwa kuyankha ku *chikonzekero changa* cha kulambira?"
- **Kudzichepetsa**. "Kodi ndine ofuna kuyimba nyimbo imene imayankhula ku zosowa za mamembala osaphunzitsidwa kwambiri a mu mpingo wanga? Kodi ndine ofunitsitsa kulalikira mwa njira yosavuta imene imafikira zosowa za mamembala osaphunzira a mpingo wanga? Kodi ndimatsogoleta ndi kudzichepetsa, kapena ndimadziona ndekha ngati wopambana pa mpingo umene Mulungu anandiikapo?" Ngati mtsogoleri wa Kulambira, machitachita anu ayenera kugwirizana ndi udindo wanu wa ubusa. Ntchito yanu yoyambirira ndi kutumikira anthu.
- **Machitachita**. "Kodi ndimafunauna njira zopangitsa kulambira kukhala kwa tanthauzo? Kodi ndimapewa kugwa mu ndondomeko zobwerezabwereza imene mwambo onse wakulambira umakhala ofanana?"
- **Mwambo**. "Kodi ndimapereka mwambo ku machitachita anga pakupewa kulakwitsa kulambira? Kodi ndimapewa kupanga mwambo ulionse wa kulambira kukhala watsopano mwakuti anthu sangaikenso chidwi chawo kwa Mulungu?"

- **Kuchita zinthu bwino**. "Kodi ndimabweretsa chopereka changa chabwino sabata iliyonse?" "Kodi ndikukula mopitiriza ngati mtsogoleri wa Kulambira?"[78]

Ndondomeko za Kutsogolera Kulambira

Mtsogoleri sangakakamize anthu kulambira; koma, mtsogoleri akhoza kuzipangitsa kukhala zosavuta kupereka chidwi chawo kukulambira.

Kutsogolera mwachitsanzo

Umodzi mwa mwayi wa kutsogolera kulambira ndi mwayi wolambira *ndi* mpingo. Mtsogoleri ayenera kumalambira pamene akutsogolera mpingo mu kulambira.

Mwatsoka, kulambira kukhoza kukhala kovuta kwa mtsogoleri. Tikhoza kukhala otangwanika kutsogolera kulambira kumene timakanika kulambira! Ngati ndinu otsogolera mayimbidwe, mukhoza kupezeka kuti nokha mukuyesa kulambira pamene muli ndi maganizo maganizo monga:

- "Oyimba nyimbo yayekha wachedwa. Ndikuona ngati kuti amabwera muno panthawi yake chifukwa cha nyimbo yapadera!"
- "Anthu sadayimbe bwino nyimbo yoyambirira. Kodi nyimbo imeneyi ndi yovuta kwa mpingo?"
- "Zikumveka ngati tikuyimba pang'onopang'ono kwambiri. Kodi ndiyimbe mothamanga vesi lotsatira?"

Ngati ndinu m'busa, mukhoza kudzipeza nokha mukuyesa kulambira pamene mukuganiza:

- "Tili ndi anthu ochepera khumi kusiyana ndi sabata yatha. Chifukwa chiyani?"
- "Kodi ndimalize uthenga ndi kuitana anthu?"
- "Nyimbo imeneyi sikugwiriza ndi uthenga wanga! Kodi ndiyenda bwanji kuchoka pa nyimbo ya kumwamba kupita ku uthenga wanga wa chiweruzo?"

Tisamalole madongosolo a katsogoleledwe ka mwambo wa kulambira kulowa mmalo mwa kulambira mmiyoyo mwathu. Pamene tikutsogolera kulambira, tizipembedza. Izi zimalimbikitsa kulambira pa mpingo. Mlaliki wina anati "Ngati otsogolera kulambira sindife **mimbulu** amene amaima pamapazi pa mpingo kuwakakamiza kulowera ku mbali imene tikufuna. Ndife **wolambira** Amene timaitanira mpingo kulowa nafe mkupezeka wa

78 Khalidwe la kuchita bwino silitanthauza kuti okhawo amene ali atsogoleri ophunzitsidwa mwa ukadaulo ndi amene angatsogolere kulambira. Harold Best akufotokozera kuchita bwino ngati "ndondomeko yakukhala bwino kusiyana ndi mmene ndinalili kale." Pakuti kulambira ndi chopereka chathu kwa Mulungu, timapitiriza kufunafuna kukhala wabwino kusiyana ndi mmene tinalili. Harold Best, *Music through the Eyes of Faith* (San Francisco: Harper Books, 1993), 108.

Mulungu.” Mpingo sulambira wotsogolera akawauza kuti alambire; amalambira otsogolera akamalambira. Wotsogolera kulambira amatsogolera powonetsa chitsanzo.

Kutsogolera ndi chilimbikitso

Susanna anali maso mpaka nthawi ya 03:00 ya mmawa kusamalira mwana wodwala. Patatha ma ola atatu ogona, anadzuka kuti akonze chakudya cha mmawa kukonzekera kupita ku tchalitchi. Anafika ku tchalitchi ali otopa chifukwa chosowa chotopa tulo, anali ogwetsedwa mphwayi chifukwa anakalipira mwana pamene anayiwala kuchotsa chidole, ndipo anali atapunguka uzimu chifukwa anali ndi nthawi yochepa ndi Mulungu sabata ino.

Abusa a Joel akufuna kuona kutengapo mbali kwambiri mu kulambira. Itatha nyimbo yoyamba, akupita ku gome, “Kodi chavuta ndi chiyani anthu inu? Tili pamaso pa Mulungu. Tikulambira Mfumu, ndipo ena mwa inu mukuoneka ngati mukadamagona kunyumba! Mukuyenera mwakhumudwa. Pezekani mu kulambira!”

Zolinga za abusa a Joel ndi zabwino. Akufuna mpingo wake ukhale olambira amachitachita, koma Sussana akumva chiyani? “Ndine wolephera ngati mayi; ndinali wa ukali pa mwana wanga. Ndine wolephera ngati Mkhristu; dzulo sindinapezeke pa mapemphero. Mulungu ndi okwiya chifukwa sindinayimbe.” Pakugwiritsa ntchito ukali ngati cholimbikitsa, abusa a Joel apangitsa kulambira kukhala kovuta kwambiri kwa Sussana.

Ngati atsogoleri a kulambira, tiyenera kulimbikitsa kulambira mmoyo wathu; tikhoza kusiya zotsatira kwa Mulungu. Ndi chisomo cha Mulungu kuti amapanga kulambira kukhala kotheka; ndi chisomo cha Mulungu chimene chimalimbikitsa kulambira kowona; ndi chisomo cha Mulungu chimene chimabweretsa mtima wolambira.

Tiyenera kulimbikitsa kulambira ndi mawu olimbikitsa, koma tisamasokoneze wolambira ndi mawu a ukali kapena kutakasa maimvaimva mwa ukadaulo. Cholinga chathu kulozera wolambira kwa Mulungu. Amalimbikitsa kulambira; kulambira sikudalira ukadaulo wathu wa katakasidwe kapena kusokoneza maimvaimva. Ife ngati watsogolera kulambira sitikusowekera kuchita ntchito ya Mulungu!

Chigawo ichi chinayamba ndi nkhani ya Sussana. Tiyeni timalize ndi nkhani yoona ya mtsogoleri wa kulambira odzichepetsa ndi wolimbikitsa. David anavutika kuti apeze achinyamata akutengapo mbali mu kulambira. Anapeza kuti anali otangwanika kutumiza ma uthenga a pa lamya kusiyana ndi kulambira. Atsogoleri ena akanayamba kulambira ndi china chake motere: “Ana inu, tili pano kulambira. Siyani mafoni ndi kuika chidwi pa kulambira. Mukusoweka ulemu kwa Mulungu!”

David anachita china chake chosiyana. Pamene oyimba magitala amayimba nyimbo ya kayaziyazi ya kulambira, David moleza mtima anati, “Pamene tikubwera pamaso pa Mulungu, ndikudziwa simukufuna kusokoneza mzanu kulambira. Tiyeni tisiye mafoni

ndi kumvetsera ku mawu a Mulungu mmawa uno." Aliyense mchipinda chino asiye foni yake. David modzichepetsa anaphunzitsa achinyamata ake kulambira.

Kulambira Kapena Kusokoneza?

Tamverani umboni wa mtsogoleri wolambira wa makono:

"Ngati msodzi, ndinapita ku tchalitchi pafupi ndi sukulu yathu ya ukachenjede… kuwunika konyezimira, nyimbo zokweza [zinali] zosangalatsa. Mtsogoleri wa kulambira anali ndi tsitsi lokonza, jinzi ndi gitala lodula kwambiri. Pamayambiriro pa mwambo wa kulambira, ndinaona maikolofoni yosagwiritsidwa ntchito yolekeza mchiuno mwake. 'Kodi ingakhale ya ntchito yanji?' Ndinakweza manja anga ndi kudzigwetsera mu zoyimba."

"Nyimbo zinali za mphamvu, gulu la mayimbidwe linali lokhazikika, ndipo nyimbo zinakonzekeredwa bwino kutsogolera kufikira nyimbo yomaliza. Pamene mtsogoleri anayimba mawu omaliza (ndagwada pansi pa mapazi anga, kupereka zonse zanga), anagwada pansi ndi mawondo ake. Ndi panthawi iyi pamene ndinazindikira cholinga cha maikolofoni amene samagwira ntchito anaika pa msinkhu wa mtsogoleri kuti azitha kuyimba ndi kuyimba gitala koma ali chogwada. Sindikufuna kuweruza cholinga cha mpingo uwu, sindingathandize koma ndikumva ngati ndinasokonezedwa kuti nditakasike ku zochita izi za maimvaimva, zimene zinakonzedwa kale nthawi isanafike."[79]

Chitsanzo ichi chikuchokera ku kulambira kwa makono, koma tikhozanso kugwiritsa ntchito zitsanzo zochokera ku kulambira kwachikhalidwe. Kuipa kwa kusokoneza ndi kusakhala ndi malire pa kalambiridwe ka mtundu umodzi. Pa kusatengera mayimbidwe athu a nyimbo kapena zolinga, tikhoza kusokoneza mpingo ngati zidole zimene tingazisokoneze ku maimvaimva ena alionse.

Kodi maimvaimva mu kulambira ndi olakwika? Ayi; timaona zitsanzo zambiri za zotsatira za maimvaimva. Ndi zolakwika kuyesa kulimbitsa kuvomereza kwa maimvaimva? Ayi; kulumikizana kwabwino kumakhudza maganizo ndi maimvaimva. Komabe ngati sitikusamala, tikhoza kupanga maimvaimva ena ake, kupatula pa ntchito ya Mzimu Woyera.

Kodi tingasiyanitse motani kutsogolera kwa kulambira ndi kusokoneza? Kusokoneza kumabwera pamene kuchitapo kanthu kwa mpingo kumabwera kumadalira pa zochitika za mtsogoleri osati Mzimu Woyera. Mwina tikhoza kusiyanitsa pakati pa kutsogolera ndi kusokoneza, koma izi ndi zizindikiro zina zimene zingawonetse kuti tikhoza kudutsa malire kupita mu kusokoneza.

1. **Tili pa chiopsezo cha kusokoneza kulambira tikamasokoneza maimvaimva ndi kulambira**. Timayamba kumva kuti ndi udindo wathu kupanga kuchitapo kanthu kwa maimvaimva. Otsogolera kulambira ena anena kuti, "Zabodza ndi kufikira

79 Joel Wentz, "Confessions of a Former Worship Leader." Zopezeka pa https://relevantmagazine.com/life5/1301-confessions-of-a-former-worship-leader/ July 22, 2020.

zili zenizeni. Namizirani maimvaimva kufikira anthu atamva kuti ndi zoona." Izi zikufanizira kuti ntchito yathu ndi kugwiritsa ntchito maimvaimva kuti apange kulambira. Otsogolera kulambira amatsogolera kulambira; sitipanga kulambira.

2. **Tili pa chiopsezo cha kusokoneza kulambira tikamayelekeza kuti mulingo wa kulambira umafunikira pa kusintha kwa mtima**. Mulungu akhoza kugwira ntchito mu mwambo wa mapemphero ndi maimvaimva, komanso akhoza kukhala ndi nthawi yachete kunyumba. Tili pa chiopsezo cha kusokoneza mpingo ngati tikhulupirira kuti ndi kudzera mu luntha lathu lokha limene Mulungu angabweretse kusintha kwa iwo amene timawatumikira.

3. **Tili pachiopsezo cha kusokoneza kulambira pamene tikamafanizira machitachita a thupi ndi kulambira**. Nthawi zina mtsogoleri amafuna anthu kuti achitepo kanthu, ndiye amati, "Ngati mumakonda Yesu, kwezani manja anu." Zachidziwikire, ndizotheka kuti wina wake m'gulumo akweza manja! Kapena, wina wake amene amakonda Yesu sakweza dzanja. Kulambira sikufanana ndi machitidwe owonekera a thupi. Kuwomba m'manja poyimba nyimbo siziwonetsa kuti tikulambira kusiyana ndi kukhala mwachete nthawi ya pemphero zimaonetsa kuti tikupemphera. Mulungu yekha amaona mtima wa wolambira. "**Wotsogolera kulambira akamawonetsera zakunja powonetsa maganizo a mkati, akuchita zolakwika.**"[80]

4. **Tili pa chiopsezo cha kusokoneza kulambira tikamafuna kuchita zimene Mulungu anachita nthawi ina kapena malo ena**. Tisamaganize kuti pakuti Mulungu anadalitsa nyimbo ina sabata yatha, adalitsa nyimbo yomweyo sabata ino. Mulungu akamagwira ntchito, amagwira mwanjira yake. Atsogoleri a Matamando azilola Mulungu kukhala omasuka kubwera m'mene wafunira. Awa simasenga amene amabweretsa mchitidwe wa uzimu pa zochitika zili zonse.

5. **Tili pa chiopsezo cha kusokoneza kulambira tikamayesa utumiki wathu ndi kuthekera kwathu kofuna kupeza chidwi chochokera kwa anthu**. Mlaliki aliyense komanso woyimba amakonda kupeza kuti anthu akuti chiyani; izi ndi zabwino. Koma tikamayesa mphamvu za utumiki wathu ndi mayankho awa, tili pachiwopsezo chodalira pa luso lathu osati Mzimu Woyera.

Mutu uwu ndi ovuta. Nthawi zambiri mawu omwewo amene ayankhulidwa pa nyengo ziwiri zosiyana amawonetsa zilimbikitso zosiyana. Mwa njira ina, ngati sitisamala tikhoza kuyamba kusokoneza kulambira. Mwa njira ina, ngati tili ndi mantha kwambiri ndi maimvaimva sitingapereke utsogoleri!

Chifukwa cha ichi, tiyenera kukhala ochedwa kuweruza utsogoleri wa kulambira wa wina wake ndi kukhala wa changu kusanthula utsogoleri wathu. Tiyenera kufunsa Mulungu kuti

80 Warren Wiersbe, *Real Worship* (Grand Rapids: Baker Books, 2000), 215.

atiwonetse zolinga zathu pakutsogolera. Tiyenera kukhala osamala kutsogolera kulambira wopanda kusokoneza wolambira ku machitidwe ena ake amene timafuna.

Mafunso Odziwika

Kodi timayamba mapemphero motani?

Chitsanzo choipa:

10:00, ndi nthawi yoyambira mapemphero. Abusa akuyesetsa kuti apeze otsogolera nyimbo. Azimayi atatu akugawana za maphikidwe. Azibambo anayi akukambirana za kusowa kwa mvula ku mbewu. Kodi tingachoke bwanji mu zinthu zonse izi kupita mu kulambira?

Umodzi mwa maudindo a mtsogoleri wa kulambira ndi kutsegulira mapemphero. Kodi tingaitane anthu a Mulungu motani pamaso pa Mulungu?

- **Mipingo ina imayamba ndi nthawi yakukhala bata**. Mtsogoleri amayamba, "Yambanafeni mu nthawi ya pemphero la bata pamene tiulowa mkupezeka kwa Mulungu."
- **Mipingo ina imayamba ndi "kuitanira kulambira" kwa nyimbo.** Iyi ikhoza kuyimbidwa ndi kwaya, munthu mmodzi, kapena ikhoza kukhala kolasi ya mpingo onse. Mu mipingo ina, abusa akhoza kupita patsogolo ndikuyamba kuyimba nyimbo monga, "Ndidzalowa mzipata zake ndi mayamiko mu mtima mwanga..."
- **Mipingo ina imayamba ndi vesi la malemba**, nthawi zambiri kuchokera ku Masalimo.

  Bwerani, tiyeni timuyimbire Yehova mwachimwemwe, tiyeni tifuwule kwa Thanthwe la chipulumutso chathu. Tiyeni tibwere pamaso pake ndi chiyamiko ndipo mupembedzeni Iyeyo ndi zida zoyimbira ndi nyimbo (Masalimo 95:1-2).

  Masalimo amene amaitanira wolambira pamaso pa Mulungu ndi Masalimo 15, Masalimo 66:1-4, Masalimo 96:1-4, Masalimo 100, Masalimo 105:1-3, Masalimo 107:1-3, Masalimo 149:1-2, ndi Masalimo 150.

Kodi zolengeza ndi kulambira?

M'busa wa Chispanish anafunsa, "Kodi zolengeza zimapezeka pati mu kulambira? Timayesetsa kukhazikika pa kulambira ndi kupezeka kwa Mulungu mu mpingo wathu. Timakhala ndi mwambo wopambana wa kulambira ndipo pamapeto pake timamaliza mndandanda wa utali wa zolengeza zotopetsa. Izi zimaononga mzimu wa mapemphero. Ndi chifukwa chiyani timapanga zolengeza kukhala mbali ya mapemphero?"

Pakusatengera pamene timaika zolengeza, zikhoza kusokoneza mapemphero. Zolengeza sikulambira kwenikweni; mmalo mwake zimasokoneza kulambira. Kodi mukhoza kutani? Palibe yankho labwino, koma maganizo ochepa akhoza kuthandiza:

- Ngati pali kuthekera, sindikizani mwakulemba zolengeza kusiyana ndikuwerenga mokweza. Pamene mukupanga zolengeza pagulu, zifupikitseni.
- Gwiritsani ntchito kanema wa pansaru kuti muwonetse zolengeza mapemphero asanayambe.
- Mipingo imakhala ndi zolengeza, nthawi ya mapemphero, kenako mwambo wa mapemphero umayamba. Pali mpingo wina umene umayamba 10:00. Mpingo uwu umachita zolengeza pa nthawi ya 9:50. Abusa anati, "Izi zimafikira zinthu ziwiri." Choyamba, zimalimbikitsa anthu kubwera msanga chifukwa sangamve zolengeza ngati Sali pano pofika 9:50. Chachiwiri, zimapangitsa anthu kukhala ndi chidwi chonse pa mwambo onse kuyambira pa mawu oyamba a mapemphero.
- Musalole zolengeza kusokoneza mzimu wa kulambira. Mmalo mwake, onani zolengeza kukhala mbali imodzi ya kukwaniritsira utumiki wa mpingo, pangani zolengeza, ndipo pitirizani. Pamene tikuona kuti zochitika za pampingo (chiyanjano cha mapemphero mapemphero a gulu, zochitika za kufalitsa ndi chitukuko cha mpingo) ndi mbali imodzi ya kulambira, kulengeza kwa zochitika izi ndi mbali imodzi ya kulambira kwa mpingo. Monga ngati mmene tate angamalizire mapemphero a banja lonse pakukumbutsa banja za chikonzero cha sabata. Zolengeza za zochitika za pampingo zimatikumbutsa kuti ndife banja; chiyanjano cha banja ndi chiganizo chofunikira cha kulambira.

ZIOPSEZO ZA KULAMBIRA: "TIMACHITA IZI CHIFUKWA..."

Mkwatibwi watsopano anali kuphika hamu cha madzulo cha pa Sabata. Asanaike hamu mu uvuni, anadula mosamula mbali imodzi ya kumapeto kwa hamu ndikuika mu chiwaya chaching'ono. Amuna ake anafunsa, "chifukwa chiyani ukutero?"

"Umu ndi mmene uyenera kuphikira hamu. Amayi anga nthawi zonse amadula kumapeto asanaphike." Mkwati watsopano anayamba kudabwa, "Kodi kudula kumapeto kwa hamu kummachita chiyani ku kukoma?" Anayimbira mayi ake kuti afunse, "kodi ndi chifukwa chiyani mumadula kumapeto kwa ham?"

Amayi ake anati, "Chifukwa agogo ako, amayi anga, amadula kumapeto kwa hamu asanaphike. Ziyenera zimathandiza kukoma. Tiwafunse."

Mkwati watsopano anaimbira agogo ake. Agogo anasiya kuphika, koma anayankha funso lawo. "Eya, ndikukumbukira chifukwa chimene ndimadulira kumapeto kwa hamu. Pamene agogo ako amuna ndi ine tinakwatirana, sitinathe kukhala ndi ziwaya zambiri. Chiwaya

chowotchera changa chinali chaching'ono. Hamu simakwanira mu chiyawa pokhapokha nditadula kumapendo"!

Kwa zaka 50 mwana wa mzimayiyu ndi mdzukulu wake anapitiriza "mwambo" umene unalibe tanthauzo. Sanafunsepo kuti, "Ndi chifukwa chiyani?"

Ngati wotsogolera kulambira, timachita zinthu osaganizira kuti "Kodi ndi chifukwa chiyani?"

Zifukwa zimene mpingo umachitira zinthu zina mwa mtundu wina:

1. **Mipingo kale inachita**. Muli phindu mu kulemekeza mu mwambo. Ngati mipingo kale inachita china chake, tisamasiye tisanafunse, "chifukwa chiyani anachita ichi?" Tikhoza kupeza zifukwa zabwino zosungira chikhalidwe; koma ngati "mipingo kale inachita" ndi chifukwa *chokhacho,* sichingakhale chokwanira.

2. **Mipingo ikuluikulu imachita**. Pali phindu pa kuphunzira kwa ena. Ngati mchitidwewo umatheka mu mipingo ina, tiyenera kufunsa, "Kodi izi ndizopindula kwa ife?" Kodi ndi chifukwa chiyani amachita? Tikhoza kupeza kuti pali chifukwa chabwino chotengera mchitidwe wa kulambira; koma ngati "mipingo ikuluikulu imachita" ndi chifukwa *chokhacho* sizingakhale zothandiza ku zochitika zathu.

3. **Anthu amayikonda**. Muli phindu mukulambira kumene kumalimbikitsa kutengapo mbali kwa anthu. Mulibe mu malemba chimene chimanena kuti, "Kulambira kwanu kukhale Komvetsa ulesi!" Tikhoza kupeza kuti nyimbo yokondedwa ya anthu athu ndi yoona ndipo ndi yokhala ndi kupembedza. Ngati ndi choncho, zimenezi ndizodabwitsa; koma ngati anthu amakonda nyimbo imene imaphunzitsa chiphunzitso chabodza, tisamaiyimbe.

4. **Imatilola kulambira Mulungu mu mzimu ndi choonadi**. Ichi ndi chifukwa chachikulu pa chimene timachita. Pakukonzekera kulambira ndi mwambo wa mapephero, tifunse, "Kodi nyimbo iyi ikutithandiza kudziwa kulambira Mulungu bwino? Kodi ndondomeko iyi ikutitsogolera pamaso pa Mulungu? Kodi kuyitanira kuguwa kungakhale njira yabwino yoyitanira anthu kuvomeraza ku uthenga uwu, kapena timalize ndi nyimbo ya matamando? Kodi tingalambire Mulungu motani mu mzimu ndi mchoonadi motani sabata ino?"

KUMALIZA: PAMENE TALEPHERA MU KULAMBIRA

Mpingo unayimba nyimbo yotsegulira mosatsimikizika. Kwaya inaphunzira, koma siinayimbe bwino mmawa umenewo. Oyimba payekha anaiwala mawu ake. Oyimba piyano anasewera mabatani olakwika. Uthenga wa abusa usawoneka kuti sumagwira kwa anthu. Mwambo wa mapemphero unali ovuta. Kodi izi zinakuchitikiranipo? Kodi mumachita chiyani mukalephera kutsogolera mapemphero?

1. Kumbukirani, kulambira konse ndi kukonzekera.

Kulambira kwathu ndi kukonzekera kulambira kwa kumwamba. Ndife anthu osayenera, ndipo kulambira kwathu sikwangwiro. "Timaitanidwa kuti tipereke zabwino zathu pa kulambira, osati kupereka ungwiro"[81]

2. Sabata ya mawa ikubwera.

Musasiye pa tsikuLolemba. Dikirani mpaka Lachiwiri kuti musanthule mwambo wa mapemphero. Mu mwambo wa mapemphero umene wafotokozedwa posachedwawu, nyimbo yotsegulira inali yosadziwika ku mpingo. Otsogolera amaganiza kuti amaidziwa nyimbo imeneyo; samaidziwa. Anazindikira china chake pa nyimbo iyi "Phunzitsani nyimbo iyi ku kwaya mpingo usanayimbenso." Phunzirani kuchokera ku zolakwika zanu, funani thandizo la Mulungu, ndipo lolani Mulungu kuti adzagwire ntchito kudzera mwa inu Sabata yotsatira.

3. Kumbukirani, Kulambira ndi chisomo.

Atsogoleri ambiri ndi ofuna dongosolo labwino; sitikwaniritsidwa. Kulambira sidongosolo la ubwino; kulambira ndi chisomo. Mulungu amagwira ntchito ngakhale kudzera mu zolephera zathu kuti akwaniritse zolinga zake. Umu ndi mmene ziyenera kukhalira.

4. Ngati tapereka zabwino zathu, sitinalephere.

Tsiku la Sabata limenelo, mtsogoleri wa kulambira anatuluka mu tchalitchi ali okhumudwa. Pamene amachoka, Timoteyo amamudikira. Timoteyo anali wamanyazi ndipo amayankhula mwa apo ndi apo, koma mmawa umenewo anati, "munayimba nyimbo yakuti 'Yesu amandikonda' pa chopereka." (Zoona, wotsogolera kulambira anadziwa zimene anayenera kuyimba – anasokoneza!) koma Timoteyo anapitiriza "ndinafunikira kumva nyimbo imene ija. Sabata ino a dokotala anandiuza kuti ndili ndi khansa; ndimafunika kuti ndikumbutsidwe kuti Mulungu amandikonda."

Ngati tapereka zabwino zathu, sitinalephere. Mulungu amagwira ntchito kudzera mu kuyesetsa kwathu kofooka kuyankhula Mawu ake kwa anthu amene timawatumikira.

» Kukambirana kwa Gulu. Onani "Kubwereza kuonanso Phunziro 8." Kodi pali mfundo zina zilizonse zimene simukugwirizana nazo? Kodi ndi mfundo ziti zimene mukuona kuti ndi zofunikira kwambri kuti mugwiritse ntchito posachedwa?

---

81 Mawu awa komanso maganizo awa mu chigawo ichi zachokera kwaFranklin Segler and Randall Bradley, *Christian Worship* (Nashville: B&H Publishing, 2006), 274-275.

KUBWEREZA KUONANSO PHUNZIRO 8

1. Kodi timakonzekera motani mwambo wa kulambira?

- Kukonzekera kwa mwambo wa kulambira kimayamba ndi kukonzekera ndi otsogolera kulambira kudzera mu mthawi ndi Mlulungu.
- Kakonzekeredwe kamathandizira kupereka ndondomeko ku mwambo wa kulambira.
- Mutu wa cholinga cha mwambo wa kulambira umathandiza kuonetsera uthenga.
- Kulinganiza kumaonetsetsa kuti kulambira kwathu kukuyankhula uthenga onse kumpingo onse.
    - Mwambo wolambira woyanjanitsa mbali zonse umawonetsera Mphamvu ya Mulungu komanso kupezeka kwa Mulungu pakati pathu.
    - Kulambira kolinganiza ndi kwa pagulu komanso kwa aliyense payekha.
    - Kulambira kolinganizika kumakhala ndi zodziwika kale komanso zatsopano.
- Kukonzekera kulambira kuyenera kukhala kwa utsogoleri onse wa mpingo.
- Kukonzekera kulambira kuyenera kuyang'ana nthawi yaitali.
- Tikhoza kukonzekera mopanda phuma chifukwa kulambira si za ife; ndi za Mulungu.

2. Kodi ndi chiyani chimene chili chofunikira pa kutsogolera mwambo wa kulambira?

- Wofunikira kwambiri pa Kulambira ndi Mulungu.
- Mpingo, otsogolera ku kulambira, ndi Mulungu onse amakumana mu mwambo wa kulambira. Atsogoleri sachita msangulutso wa kulambira wa mpingo.
- Mtsogoleri wa kulambira ayenera kulambira. Amatsogolera mwachitsanzo.
- Mtsogoleri wa matamando ayenera kulimbikitsa, osati kuweruza.
- Mtsogoleri wa kulambira ayenera kutsogolera osati kusokoneza.
- Zolengeza ziyenera kutengedwa mwa njira yoyenera ngati kungatheke.
- Pambuyo pa kukonzekera kulambira, tiyenera kuzisiya kwa Mulungu kuti alowe mu mwambo wathu wa kulambira, tiyenera kusiyira Mulungu kuti alowe mu mwambo wathu wa kulambira mu njira imene Iye akufunira kubwera.

NTCHITO YA PHUNZIRO 8

1. Mu phunziro 6 ndi 7, munasankha nyimbo ndi malemba kuchokera pa maphunziro asanu osiyana. Konzekerani mwambo wa kulambira pa ulionse wa mitu isanu. Khalani a ndondomeko mmene mungathere pakukonza mwambo ofanana, kuphatikizapo nyimbo za mpingo onse, malemba, mutu wa uthenga ndi mutu, komanso zina zili zonse zogwirizana ndi mwambo wanu wa kulambira. Gwiritsani ntchito ndondomeko imodzi kapena kuposerapo zimene zaperekedwa mu Mlozera A wa ntchito iyi.

2. Kumayambiriro a phunziro lotsatira, mudzalemba mayeso ochokera pa phunziro ili. Werengani mafunso a mayeso mosamala pa kukonzekera.

MAYESO A PHUNZIRO 8

1. Tchulani zigawo ziwiri zodziwika bwino mu ndondomeko ya kulambira zokhazikika pa uthenga.

2. Tchulani zigawo zikuluzikulu zinayi mu ndondomeko ya kulambira kutengera pa m'chitidwe wa anthu a Mulungu pa kulambira.

3. Tchulani madera atatu mu ndondomeko ya Kulambira yochokera pa Masalimo 95.

4. Kodi ndi zinthu zitatu ziti zimene tingakumbukire za kulambira kolinganizika?

5. Mu chitsanzo cha Baibulo cha kulambira, kodi omverera kulambira kwathu ndi ndani?

6. Tchulani zoyenereza zitatu za mtsogoleri wolambira wa mphamvu.

7. Kodi ndi zizindikiro zitatu ziti zakuti tikhoza kumasokoneza kulambira?

8. Lembani 2 Mbiri 5:13-14 kuchokera pakuloweza.

PHUNZIRO 9

MAFUNSO ENA

ZOLINGA ZA PHUNZIRO

1. Kuzindikira kufunikira kwa kukhala okhulupirika ku malemba pamene mukulemekeza kusiyana kwa zikhalidwe pa kulambira.
2. Kuunika kulambira molingana malemba komanso chikhalidwe.
3. Kumvetsetsa zovuta zina pamene mukuunika za mayimbidwe.
4. Kugwiritsa ntchito mfundo za Aroma 14 pa kulambira.
5. Kuzindikira kufunikira kwa kulola ana ndi achinyamata mu kulambira.
6. Kukhala tcheru la kuopa kulimbikitsa kwambiri maimvaimva kapena kukana maimvaimva mu kulambira.

KUKONZEKERA PHUNZIRO ILI

Lowezani 1 Akorinto 14:15-17.

CHIYAMBI

Warren Wiersbe analemba zimene anakumana nazo mu mpingo umene unalephera kumvetsetsa kulambira:

> "Konzekani kubwerera ku kulambira kwa madzulo," anatero mtsogoleri wa kulambira, ndi mawu komanso kumwetulira kwa mtsogoleri, wa sewero la pa kanema. "Tidzakhala ndi nthawi yosangalatsa."
>
> Mu nthawi ya maola a kumasana tsiku la Sabata ndinadabwa zimene chiganizocho chinatanthauza. "Tikhala ndi nthawi ya kukondwera" chikugwilizirana pa kuitanira

> ku phwando la chikondwerero lokumbukira tsiku lobadwa, koma nanga likugwirizana motani ndi okhulupirira a Chikhristu amene anakumana kudzalambira Mbuye wa ulemerero? Mose ndi anthu a Israel sanakhale ndi nthawi ya kukondwera pamene anasonkhana pa Phiri la Sinai…
>
> Yohane anakumana ndi chochitika china ngati zisudzo pa chisumbu cha Patmosi, koma ndi zokaikitsa ngati anali ndi nthawi yosangalala.[82]

Mu maphunziro amenewa, taona kuti kulambira ndi koposa nthawi yosangalatsa, kumaposa mwambo wina wake, komanso kumaposa zochitika Lamulungu mmawa. Kulambira ndi kupereka ulemerero kwa Mulungu umene akuyenera iye. Pa pepala, izi ndi zophweka; mmoyo weniweni zikhoza kukhala zovuta. Mu phunziro limeneli tiona mafunso kolingana ndi kulambira. Pamene mukuphunzira mafunso amenewa, kumbukirani funso lomaliza la kulambira silakuti, "Kodi ndimakonda chiyani? Kodi chimabweretsa ulemu ndi ulemerero kwa iye ndi chiyani?"

CHIPEMBEDZO NDI CHIKHALIDWE

» Fotokozani mtundu wa kulambira kwa mpingo wanu. Kodi ndi magawo ati a kulambira kwanu amene akufunsidwa mu malemba ndipo ndi magawo ati amene akulimbikitsika chikhalidwe?

"Chinthu chovuta kwambiri pa kulambira mdziko langa ndi kugwirizana kwa chikhalidwe. Mipingo yambiri ikukopera machitidwe a kulambira kuchokera kunja – kaya ndi makono kapena chikhalidwe. Anthu athu amakopera za kunja chifukwa chofuna kuyenda limodzi ndi nthawi basi., koma kaya 'chikhalidwe' kapena 'makono' kulambira kumabweretsa anthu pamodzi chifukwa ziwiri zonsezi ndizobwera. Tingalambire bwanji mu njira imene imalemekeza Mulungu ndi kulankhula ndi dziko limene tikutumikiramo?"

Chikhalidwe Kapena Baibulo?

Mkwatibwi ndi mkwati anali ochokera ku zikhalidwe ziwiri zosiyana kwambiri. Pa phwando la ukwati, zakudya zochokera ku chikhalidwe cha mkwatibwi zinaperekedwa. Pamene mbale modzi inadutsa, mkwati anafunsa, "Kodi ichi ndi chiyani?" mkwatibwi anamuuza ndipo kenaka anati, "Mdziko la kwathu, izi ndi zapamwamba." Iye anayankha monyansidwa, "Mdziko la kwathu, ndi zonyasa!" Kusiyana kwa zikhalidwe kutha kukhala ndi mavuto ake.

Tonsefe timachita kolingana ndi chikhalidwe. Chifukwa chimene enafe timadyera ndi mafoloko osati timitengo si kuti mafoloko ali a Baibulo kwambiri kapena amagwira ntchito yabwino kwambiri ayi. Amadyera mafoloko chifukwa anakula mu chikhalidwe chimene

82 Warren Wiersbe, *Real Worship* (Grand Rapids: Baker Books, 2000), 169-170.

chimagwiritsa ntchito mafoloko. Anzawo a Chikhristu mmadera ena a dziko amaona kuti timitengo nditofunikira kwambiri kuposa mafoloko.

Kulambira kwathu kumayendera chikhalidwe chathu. Madera ambiri a kulambira kwathu ndi zotsatira za chikhalidwe chathu. Wina amene anakula mu mpingo wa chikhalidwe cha America, akhoza kukonda phokoso la chitoliro. Chiwalo cha mpingo si cha Baibulo kwambiri kuposa gitala; Ndi gawo la chikhalidwe.

Ku Lesotho, mpingo umayimba mwa kuitana pakati pa mtsogoleri ndi mpingo. Mu machitidwe otere, mtsogoleri amayimba ndime ndipo mpingo umayimba ndime yotsatira. Mayimbidwe okongola chotere ndi chachidziwikire kuti samveka kwina kuli konse mu mpingo wa ku America. Ngati mtsogoleri wa mayimbidwe mu mpingo wa ku America akanayesera, mpingo ukanasokonekera. *Umodzi* ndi *kuitana/kuyankha* kuyimba ndi nkhani ya chikhalidwe osati mfundo ya Baibulo.

Pali mafunso atatu amene tikuyenera kudzifunsa pamene tikuunika machitidwe a kulambira:

1. Kodi tikusokoneza chikhalidwe ndi malemba?
2. Kodi kulambira kwathu kumatsutsana ndi malemba?
3. Kodi kulambira kwathu kungayankhule bwino motani kwa anthu mu chikhalidwe chimene Mulungu watiikamo?

Kodi tikusokoneza chikhalidwe ndi malemba?

Funso ili ndi ofunika pa kuunika ntchito ya kulambira kosiyana ndi kwathu. Mu nyengo ngati imeneyi, tionetsetse kuti tisasokoneze chikhalidwe ndi malemba. Ndi chophweka kuti ife tiwerenge mfundo za chikhalidwe chathu mu malemba ndi kukakamiza zimenezi pa aliyense kuti aliyense aziwerenga Baibulo mu njira yomweyo. Timayesedwa kuona ngati machitidwe athu ndiye a Baibulo.

Wina akhoza kunena, “Chitoliro ndicho chida choyenera pa nyimbo za mpingo. Magitala alibe malo mu kulambira.” Komabe, mmadera ambiri a dziko, chitoliro ndi chosatheka, pamene gitala ndiyofunikira kwambiri pa kuyimba. Palibe amene angatsutse kuti nyumba za mpingo za zaka za mazana awiri amagwiritsa ntchito zitoliro za mapaipi! Wina akhoza kukonda chitoliro cha paipi, koma asasokoneze zimene amakonda mu chikhalidwe chawo ndi mfundo za Baibulo.

Paul Bradshaw, wa mbiri ya kulambira waonetsera kuti ngakhale m’zaka za pakati pa mazana awiri a mpingo, kunali mitundu yosiyana ya machitidwe a kulambira. Pamene mpingo umafala, ndi zodziwikiratu kuti kulambira sikunakhalenso chimodzimodzi mmadera onse.[83]

83 Paul Bradshaw, “The Search for the Origins of Christian Worship” in Robert Webber, *Twenty Centuries of Christian Worship* (Nashville: Star Song Publishing, 1994), 4.

Kodi kukhudza kogwirika kwa funso ili ndi chiyani? Pa kuunikanso machitidwe a kulambira ena kapena pa kuchitapo kanthu pa maganizo atsopano kuchokera mkati mwa mpingo wathu, tisasokoneze chikhalidwe ndi malemba. Tisakane chiganizo pa chifukwa chochepa chakuti chikutsutsana ndi zabwino za chikhalidwe chathu. Ngati machitidwe a kulambira sakutsutsana ndi mfundo za Baibulo, kenako **tilore ena alambire munjira imene iwo akufuna.**

Izi sizikutanthauza kuti machitidwe ali wonse a kulambira ndi oyenera ku mpingo uli onse. Mtsogoleri wa nzeru wa kulambira adzatsogolera pa machitidwe amene akugwirizana ndi anthu amene akuwatumikira.

FUFUZANI

Kodi pali machitidwe ena a kulambira amene mwawakana chifukwa cha zimene mumakonda mu chikhalidwe chanu, ndipo osakhala chifukwa cha mfundo za Baibulo? Ngati ndi choncho, kodi uli ofuna kulola okhulupirira ena ufulu wa kupembedza munjira yawo, pamene sakusokoneza malemba?

Kodi kulambira kwathu kumatsutsana ndi malemba?

Funso limeneli ndilofunikira pamene tayesedwa kuikira kumbuyo mchitidwe wa kulambira chifukwa chakuti ndi woloredwa mu chikhalidwe chathu. Ngati tikuona kuti zimene zili zabwino mu chikhalidwe chathu zikutsutsana ndi malemba, **tiyenera kutsatira Malemba kusiyana ndi ziyembekezo za chikhalidwe chathu.**

Osintha anakumana ndi vuto limeneli pamene anabweretsa kusintha kwakukulu pa kulambira. Chikhalidwe cha Medieval chimati, “Anthu wamba a kulambira asawerenge Baibulo; sangalimvetse.” Wycliffe, Huss, Luther, ndi osintha ena anazindikira kuti malemba ndi a anthu onse. Chikhalidwe cha medieval chimatsutsana ndi chiphunzitso cha malemba. Osintha anaika moyo wawo pa chiswe kutsutsana ndi chikhalidwe chawo ndi choonadi cha malemba.

Ngati chikhalidwe chanu chimatsutsana ndi malemba, tiyenera tikane chikhalidwe chathu! Mawu a Mulungu ndi lamulo lathu lomaliza; sitinganyengerere kukhulupirika ku malemba ndi cholinga chofuna kufanana ndi dziko lotizungulira. Mawu a chidule a pa Aroma 12:2 amati, “Musafanizidwenso ndi makhalidwe a dziko lino koma musandulike pokonzanso maganizo anu. Ndipo mudzadziwa ndi kuzindikira chifuniro chabwino cha Mulungu chomwe ndi chokondweretsa ndi changwiro.”[84] Sitingalole dziko kuti litiike mu zochitika zake.

84 E. H. Peterson, *The Message* (Colorado Springs: NavPress, 2002).

FUFUZANI

Kodi alipo madera amene kulambira kukutsutsana ndi mfundo za malemba?

Kodi kulambira kwathu kungayankhule bwino motani kwa anthu mu chikhalidwe chimene Mulungu watiikamo?

Funso limeneli ndi lofunikira pa kufikira dziko lathu ndi uthenga wabwino. Ngati tikufuna kukhudza dziko lotizungulira ndi uthenga wabwino, kupembedza kwathu kuyenera kulankhule mu chilankhulo chimene amamva.

John Wesley anakumana ndi funso limeneli atayamba kutumikira ku midzi. Monga amzake wa Anglican, Wesley anakhulupirira kumayambiriro kuti mpingo unali okhawo oyenera kulalikirako. Pansi pa kutakasika ndi George Whitefield, Wesley anayamba kumvetsetsa kuti Ntchito Yayikulu imafunika kuti akalalikire kunja kwa mpingo.[85] Wesley anakakamizika kulingalira, "Kodi ndingalalikire bwanji momveka uthenga wabwino kwa ogwira ntchito m'migodi amene sadzalowa mu mpingo kupatula zikwati ndi maliro?" Yankho linali la kulalikira m'midzi.

Pa Epulo 2, 1739, Wesley anapita kunja kwa mzinda ndi kulalikira kwa anthu pafupipifupi 3,000 amene anasonkhana mmudzi. Ichi chinakhala chiyambi cha utumiki umene ukanasintha dziko loyankhula – Chizungu mu zaka za mazana 18.

Wesley anatsutsa mwa mphamvu kulalikira ku midzi kufikira kuti nthawi ina analankhula kuti, "Ndikanaganiza pafupipifupi kuti kupulumutsa miyoyo kunja kwa mpingo ndi tchimo ngati si kunakachitika mu mpingo." Atazindikira kuti tsankho lake linali chotchinga ku uthenga wabwino, Wesley anali ofuna kusintha machitidwe ake. Anzake a Anglican ambiri anatsutsa kusintha kumeneku. Mkati mwa mwezi umodzi wakulalikira kunja, a Bishop anauza Wesley kuti sanali olandiridwanso kulalikira m'mipingo ya Anglican. Pokhala ofuna kulankhula ku chikhalidwe chanu, kukhoza kukhala kwa mtengo wake; zinatengera Wesley kusalemekezeka pakati pa anzake a Anglican. Maitanidwe a Yesu kukhala kuunika ndi mchere ndi choyambirira chofunika kuposa zabwino zathu.

Michael Cosper akulingalira mafunso atatu pa kumvetsetsa ubale pakati pa kupembedza kwathu ndi chikhalidwe chotizungulira.[86]

---

85 Izi zikutilozera ku Funso 2 – "Kodi chikhalidwe chathu chimatsutsana ndi malemba?"

86 Michael Cosper, *Rhythms of Grace: How the Church's Worship Tells the Story of the Gospel* (Wheaton: Crossway Books, 2013), 176-179.

1. Ndi ndani amene ali pano?

Funso limeneli ikuyang'ana pa mpingo wathu; "Kodi ndi ndani amabwera ku misonkhano yathu?" Nthawi zina timakhala okhudzika kwambiri ndi kutumikira dziko kufikira kuti timalephera kutumikira ku mpingo. Kulambira kwathu chimakhala chopanda mphamvu pamene tikuyesera kukhala munthu wina amene si ife. Pakuti kulambira kuyenera kulankhula kumpingo, tikuyenera kufunsa, "Kodi pano pali ndani? Kodi ndi ndani waika Mulungu mu mpingo wathu?"

2. Ndi ndani amene analipo?

Funso limeneli likuyang'ana pa cholowa chathu. Monga okhulupirira, tili ndi cholowa kuchokera ku mbuyo ku mpingo woyamba ndi kutamabasukira dziko lonse.

Izi zikutanthauza kuti tidzayesetsa kubweretsa nyimbo zakale mbadwo wathu. Zikutanthauza kuti tidzalumikizitsa anthu a lero ndi mbiri ya mpingo. Akhristu a chichepere akuyenera kudziwa kuti ali gawo la cholowa chimene chinayamba kale kale tisanabadwe ndipo chipitilira ife titapita. Ndife gawo la mpingo wa dziko lonse opangidwa ndi okhulupirira ochokera ku mibadwo yonse.

Cholowa chathu cha kulambira chikupita kumbuyo ku Pentekoste, kumbuyo ku vumbulutso la Mulungu kwa Mose pa Phiri la Sinai, ndipo pa mapeto pake kumbuyo ku vumbulutso la Mulungu kwa Adamu ndi Hava m'munda wa Edeni. Kulambira kwathu kukondwerere mbiri imeneyi. Tikamayimba "Linga la mphamvu ndi Mulungu Wathu," tikulumikizana mu Kusintha. Pamene tikuyankhula Chikhulupiriro cha Atumwi, tikulumikizana mu kulambira kwa zaka za mazana awiri. Mu kulambira timafunsa, "Kodi pano panali ndani ife tisanabwere?"

3. Ndi ndani amene akufunika kukhala pano?

Funso limeneli likuyang'ana pa dera lathu. Pamene tikufunsa, "Kodi ndi anthu ati amene akuyenera kukhala gawo la mpingo wathu," timafunsa mafunso ngati:

- Ndi ndani amene tikuyesera kumufikira ndi uthenga wabwino?
- Ngati anthu a dera lathu akanabwera ku mpingo, kodi kulambira kwathu kukanaoneka motani?[87]
- Kodi tingakhale owona motani ku uthenga wathu pamene tikupembedza mnjira imene ikuyankhula kwa anthu amene tikuyesera kuwafikira?

87 John Wesley anakumana ndi nkhani imeneyi. Anglican anazindikira kuti misonkhano ya kulambira imene kumapita anthu ogwira ntchito m'migodi, imatembenuza mahule, ndi ogulitsa mu masitolo imakhala yosiyana ndi kulambira kovomerezeka kwa Anglican apamwamba. Ansembe ambiri anati salola kuti kulambira kwawo kusokonezedwe ndi anthu a pansi. Izi zinapangitsa chiyambi cha magulu a Methodist.

Mafunso awa ndi ovuta mmoyo weniweni kusiyana ndi pa pepala! Onani madera anayi awa. Mpingo uli onse wakumana ndi chovuta cha kulankhula ku dera.

Mpingo A: Mpingo umene unalephera kufunsa, "Kodi pano pali ndani?"

Mpingo A uli mu dera la anthu opuma. Ndipo zaka zakubadwa kwao zili mu ma 70, komanso zaka za opezeka kwenikweni mu mpingo zili pakati pa 70. Zaka ziwiri zapitazo, abusa awo anatsimikizika kufikira mabanja achichepere. Mu miyezi iwiri, anabwezeretsa chitoliro, kwaya, nyimbo ndi magitala, gulu la matamando, ndi kanema wa mmwamba.

Mwatsoka, abusa anaiwala kufunsa, "Kodi pano pali ndani?" Zotsatira zake, mpingo wa anthu akulu 100 watsika kukhala mpingo wa anthu 35 akulu kuyimba nyimbo sakonda, komanso kudandaula za magitala okweza.

Kodi mpingo A uzikafikira kunja? Kwambiri! Koma anthu amene angawafikire kwambiri ndi akulu-akulu amene sapita ku mpingo okhala mu dera lawo. Pa kusalabadira za anthu amene akupezeka kale mu mpingo, akulephera kupembedza mu njira imene ikulankhula ku mpingo kapena dera lozungulira. Mpingo A unalephera kufunsa, "Kodi pano pali ndani?"

Mpingo B: Mpingo umene unalephera kufunsa, "Kodi pano panali ndani?"

Mpingo B uli mmzinda umene ukukula mwa changu kukhala ndi mabanja achichepere ochuluka. Mpingo umalankhula chilankhulo cha dera lawo; chipembedzo chawo ndi chokondweretsa komanso cha changu.

Mpingo B uli ndi njala ya usodzi. Mwatsoka, Mpingo sunafunse, "Kodi *pano* panali ndani?" Mpingo B waiwala cholowa chake monga mpingo umene unalalikira uthenga wa mtima olungama komanso moyo wa Chikhristu wa chigonjetso. Abusa amapewa kulalikira chiphunzitso chifukwa akuganiza, "Anthu sakufuna kumva chiphunzitso; akufuna mauthenga amachitachita." Mtsogoleri wa mayimbidwe akupewa nyimbo za mawu okhala ndi zakuya za Baibulo chifukwa akuganiza, "Anthu sakonda nyimbo zovuta, amakonda nyimbo zosavuta." Zotsatira zake, mpingo wakuza mbadwo wa "akunja obatizika."[88]

Mpingo B ukukula mu chiwerengero, koma ma membala ake ochepa akukula mu umulungu. Anthu ambiri akupitako chifukwa ndi mpingo osangalatsa umene umafunsa kudzipereka kochepa. Chifukwa mpingo B ulibe chidwi ndi cholowa, Otembenuka mtima amachoka msanga kupita ku mipingo ina imene imapereka zosangalatsa zabwino. Mpingo B unalephera kufunsa, "Kodi pano panali ndani?"

88 Mmene Mark Dever anawatchulira Akhristu amene alibe maziko a Baibulo.

Mpingo C: Mpingo umene unalephera kufunsa, “Kodi ndi ndani akuyenera kukhala pano?”

Mpingo C Unayamba pafupifupi zaka 100 zapitazo mdera la kumudzi. Chipembedzo, ulaliki, ndi nyimbo zopita kwa anthu amene amakhala mtawuni imeneyi. Mu zaka za kulowerera, dera lasintha kwambiri. Mpingo C tsopano wazunguliridwa ndi mzinda wamkati, koma chipembedzo chake chinakonzeredwa kukopa anthu akumudzi ochita bwino pang’ono.

Mwa chisoni, anthu ambiri amene amakhala pafupi ndi mpingo C amadutsa sabata ili yonse osadziwa kuti mpingo C uli ndi yankho la njala yawo yozama. Mpingo C uli ndi uthenga umene dera lake likufuna, koma sumadzifotokozera momveka bwino ku deralo. Ngati mpingo C ukanapembedza mu njira imene ikanalumikiza Mulungu ndi dziko la zosowa, ukanasintha dera lake. Mmalo mwake, Mpingo C ukufa chifukwa cha kulephera kufunsa, “Kodi ndi ndani akuyenera kukhala pano?”

Mpingo D: Mpingo umene umalankhula ku dera

Mpingo D ukugawana zochitika zake ndi mipingo itatu ya kumbuyo. Dera lasintha kwambiri kuyambira pamene mpingo unadzalidwa zaka 40 zapitazo. Mosiyana ndi mipingo ina mu kafukufuku wathu, Mpingo D waphunzira kulumikizana bwino ndi dera.

Pamene gulu la abusa lazindikira kuti otembenuka ambiri a chichepere samamvetsetsa chiphunzitso Lamulungu, anapanga magulu a maphunziro kubweretsa okhulupirira atsopano kuti akhwime. Pamene mtsogoleri wa mayimbidwe wazindikira kuti mayimbidwe sanalankhule kwa ambiri mdera lake, anayamba kuonjezera nyimbo zimene ndi zoona mu chiphunzitso komanso za makopedwe mu mayimbidwe.

Pamene mpingo umakula, anadzala mipingo yaying’ono mmatawuni ozungulira ndi kulola mipingo imeneyi kuzolowera zosowa za madera awo. Mipingo imeneyi kutsogoleredwa ndi abusa achinyamata amene anali gawo la Mpingo D. Mpingo uli wonse waung’ono ndi osiyana, koma mpingo uli onse ndi okhulupirika ku uthenga wabwino. Mpingo D ukupambana chifukwa waphunzira kufunsa, “Kodi pano pali ndani, Kodi pano panali ndani, komanso kodi ndani akufunika akhale pano?” Waphunzira kulankhula choonadi cha Baibulo ku dera limene Mulungu wakhazika.

FUFUZANI

Kodi chipembedzo chanu chimalankhula kwa anthu amene amabwera ku mpingo? Kodi kupembedza kwanu kumaonetsera cholowa cha mpingo wa Chikhristu? Kodi chipembedzo chanu chimalankhula kwa iwo amene Mulungu amafuna kufikira kupyolera mu mpingo wanu?

Kodi Mayimbidwe Bwanji?

Amayimbidwe mu mpingo mmadera ambiri a dziko akukumana ndi vuto la kupeza nyimbo zimene ndi zomveka kolingana ndi Baibulo komanso zosakhumudwitsa mchikhalidwe. Timafunafuna nyimbo zimene zimalankhula chilankhulo cha mtima wa dera limene tikufuna tikafikire. Nyimbo za kunja si zikhala zogwirizana mu chikhalidwe, ndipo zinanso za chikhalidwe si zikhala za Baibulo. Kodi timasankha motani nyimbo zimene ndi zokhulupirika ku malemba komanso zogwirizana ndi chikhalidwe chimene tikutumikiramo? Awa ndi mayankho kuchokera kwa abusa amene anakumana ndi vuto lotere:

Pa kusankha nyimbo za mpingo, wina sayenera kusankha pakati pa kukhala zokhulupirika ku Baibulo komanso zomveka mu chikhalidwe. Ndi "kukhulupirika ku Baibulo" ndikufuna nyimbo zimene ndi zoona komanso zomveka. Ndi "kumveka muchikhalidwe" Ndi kufuna nyimbo zimene ndi zoyimbika komanso zokhudza ku mpingo.

Kukhulupirika kwa Baibulo kumatengera zoyambirira, koma sitiyenera kusankha pakati pa zimenezi. Ngati gawo la cholinga cha kuyimba ndi kusankha chilankhulo cha mayimbidwe chimene ndi chogwirizana ndi chikhalidwe [dera] la mpingo wathu? Ndife [opusa] ngati tikuganiza kuti kugwirizana ndi chikhalidwe ndi kosafunikira, komanso tidzakhala osagirizana ngati nyimbo zathu si zoona kapena zosamveka.

(Murray Campbell, mbusa ku Melbourne, Australia)

Pa kuphunzitsa abusa a ku Africa, timalimbikitsa kupeza zimene zili zodzaza ndi malemba, phata lake ndi Mulungu, za uthenga wabwino, zomangirira, nyimbo zoyimbika zimene angathe kupeza, zakale ndi zatsopano, ndi kuzisiya choncho! Mu chikhalidwe chilichonse, anthu a Mulungu akufunika nyimbo zimene zidzawaphunzitsa kukhala moyo ndi kufa chifukwa cha Khristu.

(Tim Cantrell, mphunzitsi ku Johanesberg, South Africa)

Zisudzo za umulungu zolimba, potengera nyimbo zogwirizana mu Hindi ndi zochepa kwambiri. Nyimbo zambiri zimene zili ndi chiphunzitso chabwino cha umulungu zatanthauzidwa kuchokera ku nyimbo zakale za azungu kapena nyimbo za chipembedzo cha makono. Ngakhale mawu akhoza kukhala okhulupirika, mayimbidwe si a muchikhalidwe, ndipo anthu a mu dera amavutika kuyimba. Komanso, nyimbo zotere zimangotsindika chikaiko cha anthu kuti Chikhristu ndi chipembedzo cha azungu.

Mwanjira ina, nyimbo za chi Hindi zimene mayimbidwe ake akutengera nyengo, kawirikawiri ndi zopepuka ku chiphunzitso cha Mulungu, zobwerezedwa, ndi zopanda Malemba Nthawi zina nyimbo zimatenga mayimbidwe amene amagwiritsidwa ntchito mmakachisi. Timapewa mitundu iwiri yonseyi ya nyimbo.

Chinthu choyamba chimene ndimayang'ana pa kusankha nyimbo ndi kukhala ndi chiphunzitso chovomerezeka. Ngati nyimbo ndi yosamveka pa chiphunzitso cha Mulungu, sitiyimba, kaya ikhala ya nyengo yotani. Ngati mawu ake ndi abwino koma mayimbidwe ake si aku India, sitiyimba, Timasankha nyimbo zokhala ndi mayimbidwe a ku India komanso mawu okhulupirika. Zamveka, si nyimbo zambiri zimene zikupezeka mu chigawo chimenechi, koma pang'ono pang'ono tikumanga kuthekera kwathu.

(Harshit Singh, mbusa ku Lucknow, India)

Monga kuli chilankhulo cha mtima chimene munthu amalankhula mwa chilengedwe ndipo chimamveka mwakuya, pali chilankhulo cha mtima wa mayimbidwe chimene chimalankhula kwa munthu mwakuya.

Ganizani za mtumwi amene amalephera kuphunzira chilankhulo cha anthu kumene akutumikira. Akhoza kunena kuti (mchilankhulo chake) "Ndiri pano kukupatsirani uthenga wabwino. Simungamvetsetse zimene ndikunena, koma pitirizani kumvetsera. Mapeto pake, mudziwa chimene ndikuyankhula ndipo mudzadziwa uthenga wabwino." Si choncho! Chimodzimodzi, pamene talephera kugwiritsa ntchito chilankhulo cha mayimbidwe cha chikhalidwe, tikupanga uthenga wabwino kukhala ovuta kwambiri kumvetsetsa.[89]

Za chisoni, monga abusa a Singh analemba, mu zikhalidwe zina muli nyimbo zochepa za mphamvu za Baibulo zimene zimagwiritsa ntchito chilankhulo cha mayimbidwe chimene si cha Chizungu. Kawirikawiri izi zimapangitsa mpingo kutsala ndi zisankho ziwiri: nyimbo za mphamvu za Baibulo za mayimbidwe ndi kamvekedwe ka chilendo kapena zofooka kulingana ndi Baibulo koma nyimbo zokhala ndi mayimbidwe amene akutengera nyengo. Ngati tikufuna kugwiritsa ntchito mayimbidwe kumanga mpingo pa dziko lonse, tifune mayimbidwe amene ali oona ku malembo ndipo amalankhula ndi mmtima wa chiyankhulo cha mayimbidwe anthu. Ndikukhulupirira kuti Mulungu akufuna kuitana anthu olemba nyimbo za umulungu mu chikhalidwe chilichonse.

---

89 Chitsanzo ichi chatengedwa mu Ronald Allen and Gordon Borror, *Worship: Resdiscovering the Missing Jewel* (Colorado Springs: Multnomah Publishers, 1982), 168.

Ngati mutumikira mu chikhalidwe chimene mukupezeka mayimbidwe a pamwamba ochepa, mukhoza kulimbikitsa mayimbidwe atsopano. Izi zikhoza kufunika kugwirizana pakati pa anthu awiri; wina olemba kapena kutanthauzira ndime za pamwamba ndi wina olemba nyimbo. Ndi olemba nyimbo ochepa chabe amene analemba nyimbo zawozawo. Pezani Mkhristu odzipereka ndipo alembe mayimbidwe a nyimbo zimene zikulankhula za choonadi cha Baibulo. Pakuchita zimenezi, mukhoza kuyimba uthenga wa Baibulo mu chilankhulo cha nyimbo chimene chimalankhula ku dziko lanu.

Nthawi zonse tikuyenera kulingalira Funso 2 pamwamba: "Kodi chikhalidwe chathu chimatsutsana ndi malemba?" Ngati chikhalidwe cha mayimbidwe athu chikutsutsana ndi malemba, tisachigwiritse ntchito. Komabe, pamene palibe mfundo ya Baibulo, tifunefune kutsogolera chipembedzo muchilankhulo cha mayimbidwe cha opembedza.

Pamene tikupembedza mu mpingo wa atate wake, wachinyamata wina amene amakonzekera utumiki anazindikira kuti anthu ochepa amamvetsetsa nyimbo zimene amayimba. Mmalo mopembedza, anaonetsera kumvetsetsa kochepa kwa choonadi chimene amayimba. Pamene wachinyamata uyu anadandaula za zimenezi, atate wake anayankha, "Taona ngati ungachite bwino." Isaac Watts anavomera chilimbikitso cha atate wake.

Anthu – olankhula Chizungu lero akuyimba nyimbo za Isaac Watts chifukwa mbusa wachinyamata uyu anatsimikizika kulemba nyimbo zimene zimafotokoza uthenga wabwino mu chilankhulo chimene anthu amamvetsetsa.[90] Mbadwo wathu, tikufunika olemba nyimbo amene amalankhula choonadi cha Baibulo mu zilankhulo zimene zimakhudza mitima ya dziko limene sililankhula Chizungu.

MAGANIZO ENA OMALIZA PA MACHITIDWE A MAYIMBIDWE

Chifuwa mayimbidwe ndi gawo lofunikira mmoyo, ambiri a ife tili ndi zikhulupiriro za mphamvu zokhudza mayimbidwe. Kukambirana kuli konse kwa machitidwe a mayimbidwe mu chipembedzo kumatha kuyambitsa makangano.

Amene amakhulupirira kuti machitidwe ena a mayimbidwe ndi oipa amati, "Machitidwe ena ake ndi okhawo amene akhoza kugwiritsidwa ntchito mu chipembedzo." Komabe, malemba sakupereka ndondomeko zapadera za machitidwe a mayimbidwe.

Amene amakhulupirira kuti machitidwe a mayimbidwe alibe mbali pa umunthu, amanena, "Pezani nyimbo zimene anthu amakonda ndipo yimbani zimenezo; imbani zimene mumakonda.'' Komabe, malemba amanena poyera kuti pipewe chilichonse chimene chingathe kutsogolera ku machitachita a thupi. Chifukwa cha kufunikira kwa chikhalidwe ndi maimvaimva, mayimbidwe ena ndiosafunikira mu chipembedzo.

---

90 "Chikondwerero ku Dziko," "Ndikafufuza," ndi "O Mulungu, Thandizo mu Kuyambira Kale'' ndi nyimbo zitatu mwa 750 zolembedwa ndi Isaac Watts.

Kulemba za chisankho cha mayimbidwe, Scott Aniol anagawa zokambirana mmagawo awiri:[91]

1. **Uthenga: nkhani yabwino ndi yoipa.** Posatengera machitidwe a mayimbidwe, ngati uthenga sukukamba choonadi momveka bwino, ndi yosayenera pa kulambira. Iyi ndi nkhani ya chabwino ndi choipa. Pali nyimbo zambiri zogwiritsa ntchito mayimbidwe a chikhalidwe zimene zili ndi mauthenga amene saphunzitsa choonadi cha Baibulo; izi ndi zosayenera pa kulambira. Pali nyimbo zambiri zimene zimagwiritsa ntchito mayimbidwe machitidwemakono amene ali ndi mauthenga amene saphunzitsa choonadi cha Baibulo; awa ndi osayenera pa kulambira.

2. **Mtundu wa Mayimbidwe:** Pakuti malemba sanena momveka pa nkhani ya mtundu wa mayimbidwe, titsatire mfundo za Aroma 14. Tipewe mayimbidwe amene ndi opatsa mafunso chifukwa cha kulumikizana pa zikhalidwe. Komabe, tisaweruze ena amene chikumbumtima chawo chikuwatsogolera ku mbali zosiyanasiyana za mayimbidwe.

FUFUZANI

Kodi mu chipembedzo chanu muli madera ena a chikhalidwe amene amaika malire kuti musafikire dziko lanu ndi uthenga wabwino? Kodi ndinu okonzeka kutaya zimene mumakonda kuti mufikire dziko lanu ndi uthenga wabwino?

Nanga Kuomba mu Manja?

Kodi kuomba mu M'manja nthawi ya chipembedzo bwanji? Kodi ndi zolondola kapena zoipa? Kuomba mu manja kumachitika mmagawo awiri, ndi matanthauzo awiri osiyana.

Kuomba mu M'manja ngati gawo la kulambira

Mipingo yambiri imaomba mu manja monga gawo la mayimbidwe. Kuomba M'manja ndi awo la kulambira kwa mpingo wawo. Ili ndi gawo la thupi pa kulambira monga malemba akufotokozera. "Ombani mu manja, inu anthu onse; fuwulani kwa Mulungu ndi mawu achimwemwe!" (Masalimo 47:1). Olambira a Chiyuda anali a changu. Kulambira kwa Chiyuda kunali ndi mitundu ya zida za maimbidwe, kukweza manja, komanso kuomba mu M'manja.

91 Scott Aniol, *Kupembedza mu nyimbo* (Winona Lake, IN:BMH Books, 2009), 135-140.

Ngati kuomba mu M'manja ndi gawo la kulambira kwanu, mtsogoleri wa kulambira awonetsetse kuti ndizoyenera ndi nyimbo imene ikuyimbidwa. Kuomba mu manja nthawi ya nyimbo ya pemhero sikugwirizana ndi uthenga. Kuomba mu manja nthawi ya nyimbo ya kulemekeza mokondwera ndi koyenera. Funso la mtsogoleri nthawi zonse lisakhale lakuti, "Kodi kuomba mu manja ndi koyenera kapena kolakwika?" Funso la bwino likhoza kukhala lakuti, "Kodi kuomba mu manja ndi koyenera pa nyimbo iyi komanso pa gawo limeneli la kulambira?"

Kuomba mu M'manja pa kuchitapo kanthu pa kulambira

Nkhani yovuta kwambiri ndi kuomba mu manja *pa kuyankhapo* pa nyimboya padera. Palibe chionetsero mu malemba pamene opembedza a Chiyuda kapena a Chikhristu anaomba mu manja pa kuyankhapo pa chipembedzo.

Zikhalidwe zina lero, ndi za changu kuomba mu M'manja pa kuonetsera kuyamika. Mu zikhalidwe zotere, ndi zosavuta kuomba mu manja pa kutamanda Mulungu kupyolera mu kuomba mu manja. Zikhalidwe zina zimaomba mu manja ndi cholinga choyamba cha kuonetsera kuchita bwino. Mu zikhalidwe zotere, kuomba mu manja pa kuyankhapo pa kwaya kapena oyimba kukhoza kupangitsa maganizo a magule, mmalo mwa kulambirra.

Pakuti malemba sakukamba nkhani imeneyi mwa chindunji, tipewe kulankhula kwa ntheradi. Ngati kuomba mu manja ndi njira ya chikhalidwe ya kuonetsera matamando kwa Mulungu, ikhoza kukhala mchitidwe wa kupembedza. Ngati kuomba mu manja kukuonetsera, "Munthu uyu wachita bwino ndi kutikonderetsa," ingasokoneze kulambira.

Mpingo ndi oyimba onse awone cholinga cha kuomba m'manja. Anthu mu mpingo adzifunse okha, "Kodi ndi chifukwa chiyani ndi kuomba mu manja? Kodi kuomba m'manja kwanga kukuchokera mu matamando kwa Mulungu kapena kutamanda amene akuyimba?"

Oyimba afunse, "Kodi ndi chifukwa chiyani mpingo ukuomba m'manja? Kodi nyimbo yanga inalimbikitsa machitidwe a chikondwerero a kutamanda Mulungu, kapena nyimbo yanga inabweretsa chidwi pa luso langa? Kodi ndinatsogolera mwa kupembedza" Monga atsogoleri a kulambira tikuyenera kusamala kuti utumiki wathu uloze kwa Mulungu, osati ku kuthekera kwathu.

FUFUZANI

Mu mpingo wanu nthawi ya kulambira, kodi ndi kuonetsera matamando kwa Mulungu kapena kuonetsera matamando kwa oyimba?

Aroma 14 ndi Mitundu ya Kupembedza

» Werengani Aroma 14:1-23.

Aroma 14 akutipatsira mfundo zofunikira pa mafunso amene malemba sakulankhula mwa chimvekere. Paulo akulankhula kwa iwo amene sakugwirizana ndi kudya nyama kapena kutsatira masiku ena apadera. Akupereka mfundo zimenezi.

1. Musaweruze ena za zinthu zokaikitsa (Aroma 14:1-13).

Mmadera amene malemba sakulankhula mwa chimvekere, tikuyenera kulola ufulu wa maganizo kwa iwo amene sakugwirizana ndi ife. Sitiyenera kukhala okhazikitsa kuposa malemba eni!

2. Musakhumudwitse ofooka (Aroma 14:13-15).

Paulo anazindikira kuti okhulupirira osakhwima akhoza kuvulazidwa ndi maufulu amene okhulupirira okhwima akuchita. Potero, Lamulo la chikondi likutifunsa kuti tichepetse maufulu athu chifukwa cha ofooka. Musaononge amene Khristu anafera chifukwa cha ufulu wanu.

Chiganizo cha Paulo ndi chitsanzo cha mphamvu cha madera onse a chikhalidwe cha Chikhristu; "N'chifukwa chake ngati zimene ine ndimadya zichititsa m'bale wanga kugwa mu tchimo, sindidzadyanso chakudyacho kuti m'baleyo ndisamuchimwitse" (1 Akorinto 8:13).

3. Chitani mwa chikhulupiriro, osati mwa kukaikira (Aroma 14:23).

Iyi ndi mfundo yofunikira kwa Akhristu a chichepere. "Koma munthu amene akukayika atsutsidwa ngati adya, chifukwa kudya kwake si kwa chikhulupiriro; ndipo chilichonse chosachokera m'chikhulupiriro ndi tchimo."

Tikachita kuchokera ku mitundu ya chipemebdzo, mfundo izi zimatichenjeza:

1. **Musaweruze amene akugwiritsa matundu umene inu simukondwera nawo**. Ngati malemba sakukamba mwa chimvekere, musafulumire kuweruza.

2. **Musagwiritse ntchito mayimbidwe amene akhoza kukhumudwitsa okhulupirira watsopano**. Ngati okhulupirira akuchokera ku chikhalidwe chimene mtundu wa mayimbidwe ena akufanizidwa ndi chikhalidwe choipa, mtundu umenewo *sungakhale* othandiza kwa okhulupirira ameneyo. Chikondi cha pa mbale wa Chikhristu chikulimbikitseni kupewa chili chonse chimene chingathe kutchinga kukula kwa uzimu wake.

3. **Musachite ufulu wanu pamene chikumbumtima chanu chili ndi chikaiko**. Musamakaike. Chikondi cha Mulungu chikulimbikitseni kupewa chilichonse chimene chikuyambitsa chikaiko mu chikumbumtima chanu.

KUBWERETSA PAMODZI ANA NDI CHINYAMATA MU KULAMBIRA

"Kodi tingabweretse bwanji ana ndi achinyamata mu kulambira? Kodi tiwaike mu msonkhano waokha kufikira atakula kuti amvetsetse kulambira kwa akulu? Kodi tingalimbikitse bwanji ana ndi achinyamata kuti apembedze ndi choonadi?"

Mipingo yambiri imasiyanitsa ana, achinyamata komanso akulu mu kulambira. Pali zifukwa ziwiri pamenepa: Kukhudzika kwakuti ana ang'ono asokoneza akulu pa kulambira komanso kukhudzika kuti achinyamata samvetsetsa zimene zikuchitika mu mwambo wa kulambira.

Palibe choletsa mu malemba choletsa kusiyanitsa mapemphero a chinyamata kapena ana. Komabe pali zinthu zitatu zimene ziyenera kulingalirapo:

1. **Mu malemba, kulambira ndi kopatsirana pa mibadwo.** Malemba sakunena kuti ana ndi achinyamata anachitiridwa mosiyana mu kulambira. Mu kulambira kwa Kachisi, banja limakhala pamodzi pa mwambo wa nsembe. Palibe chinthu mu Chipangano Chatsopano chimene chikuonetsa kuti mpingo woyamba umalekanitsa ana kapena achinyamata nthawi ya kulambira.

2. **Kulambira kopatsira m'badwo wina kumabweretsa mgwirizano mu Thupi la Khristu.** Monga chopereka chimasiyanitsa mapemphero a kulambira kwa makono ndi kulambira kwa chikhalidwe kukhoza kuchepsa umodzi wa Thupi, chopereka chimatha kusiyanitsa mapemhero a ana ndi achinyamata kukhoza kuchepetsa chidziwitso chawo cha kukhala gawo la banja la mpingo. Mbali ina, monga ana ndi achinyamata akuikidwa pamodzi mu kulambira kwa banja la mpingo, aliyense amamvetsetsa kuti ndi gawo lofunikira la Thupi la Khristu (1 Timoteyo 4:12).

3. **Kudzera mu kulambirakopatsira m'badwo wina, chikhulupiriro chimapatsidwa kwa mbadwo wotsatira.** Timaphunzira pa kulambira Pokhapokha ngati pali dongosolo la bwino, mapemhero a ana akhoza kukhala nthawi ya kusangalatsa ana kuti asasokoneze mapemhero a akulu. Tikachita motere, ana aphunzira liti kupembedza?

Achinyamata ndi Ana ndi Monga Gawo la Mapemphero a Kulambira kwa Umodzi

Achinyamata ndi ana akhoza kukhala nawo mu mapemphero a kulambira kwa umodzi amene amayankhula kwa mibadwo yonse. Izi zikhoza kukhala ndi uthenga waufupi wa ana pa mutu omwewo ngati uthenga waukulu.

Ngati tikuganiza kuti ana sangamvetsetse choonadi chakuya, tidzalephera kuwapatsa malikisi oyenera pa chidziwitso cha uzimu. Ndi Mzimu Woyera amene amaunikira omvera aliyense, wamkulu kapena mwana (1 Akorinto 2:10). Ngakhale mu mapemphero akulu, Mzimu Woyera akhoza kulankhula choonadi ku mitima yawo yachichepere. Kuvomereza ana mu kulambira kwa akulu kukufunika kuwaphunzitsa za kulambira. Tikhoza kufotokozera utumiki kwa ana. Tikhoza kutanthauzira mawu ovuta mu malemba owerenga komanso nyimbo. Ngakhale akulu nthawi zina amafunika mawu amenewa atanthauziridwe! Pakupereka mpata kwa ana mu kulambira, timalola iwo kuti akule ngati wolambira pambali pa thupi lawp lonse.

Patulani Kulambira kwa Achinyamata ndi Ana[92]

Mipingo yambiri imapereka utumiki wapadera wa achinyamata ndi ana. Utumiki umenewu ukhale kupembedza, osati zosangalatsa. Ngati ana ndi achinyamata saphunzira kupembedza, sangakule mpaka kukhwima mu uzimu. Monga mwana sakula mu thanzi la ku thupi ndi maswiti, la uzimu ndi chakudya choperewera cha uzimu.

Ngati mpingo ukulekanitsa utumiki wa akulu ndi achinyamata /ana tionetsetse kuti utumiki ndi wa kulambira weniweni. Kulambira kwa achinyamata ndi ana kukhale ndi kuwerenga mawu. Kwa ana, zithunzi zopatsa chidwi zikhoza kulimbikitsa choonadi cha malemba.

Utumiki ukhale ndi uthenga kapena phunziro la Baibulo la mawu a Mulungu limene likufikira zosowa za achinyamata ndi ana. Baibulo pa lokha ligwiridwe ndi chikondi mu manja mwa mphunzitsi. Ana ndi achinyamata phunzirani kulemekeza ndi kugwiritsa ntchito Mawu a Mulungu pa kuonera akulu amene amawalemekeza akugwiritsa ntchito.

Utumiki ukhale ndi nyimbo zimene zikukamba choonadi cha Baibulo. Mukhalenso nthawi ya pemphero, matamando ndi mapembedzero zonse. Mukhalenso chopereka chimene chimalola ana kubweretsa mphatso kwa Mulungu. Zinthu zonse za kulambira zikhale muutumiki wa kulambira wa ana kapena achinyamata.

---

92 Chigawo chimenechi chimagwiritsa ntchito ya Mrs. Christina Black, Professor of Education ku Hobe Sound Bible College.

KUPHUNZITSA ANA KUPEMPHERA: "DZANJA LA PEMPHERO"

Chala chachikulu chimatikumbutsa kupemherera amene ali pafupi ndi ife (banja).

Chala cholozera chimatikumbutsa kupempherera amene amalozera anthu kwa Yesu (abusa, aphunzitsi, ndi atumwi).

Chala chapakati ndi chachitali pa zonse. Ichi chimatikumbutsa kupeherera atsogoleri a dzko lathu, sukulu, mpingo ndi kwathu.

Chala chachinayi ndi chofooka pa zonse. Onetserani izi pa kuyesera kukweza chala chachinayi chokha. Izi zikutikumbutsa kupempherera iwo amene ali ofooka komanso akufunikira Yesu.

Chala cha chisanu ndi chaching'ono pa zonse. Izi zikutikumbutsa kudzipempherera wekha.

Kukweza **dzanja lonse** kumatikumbutsa kutamanda Mulungu.

Dzanja la Mulungu limeneli lasanduka njira ya pemphero imene imakweza mlingo wa opembedza achichepere.

Pomaliza

Ngati tikufuna kuona ana athu kukula kukhala okhulupirira okhwima, tikuyenera kupereka kwa iwo chakudya cha uzimu. Kaya mu utumiki wa umodzi kapena wosiyana, titsogolere ana athu ku kulambira.

FUFUZANI

Kaya muli ndi mapemphero apadera ana ndi achinyamata kapena mapemphero a umodzi a mpingo onse, kodi mukuphunzitsa ana anu ndi achinyamata kupembedza?

MAIMVAIMVA MU KULAMBIRA

"Anthu a dziko langa ndi a maimvaimva kwambiri, ndipo kupembedza kwathu kumaonetsera moyo wathu wa maimvaimva kawiri kawiri. Nyimbo zathu za kulambira ndi za changu nthawi zambiri, zokweza, komanso zokweza. Zimalola kuti tichite ndi kuonetsera maimvaimva athu. Komabe, ndimaopa kuti nyimbo ***zokha*** *maimvaimva. Sindikudziwa ngati nyimbo zathu zimatsogolera ku kulambira."*

Kulambira koona ndi kulambira kwa mumzimu ndi choonadi. Chipembedzo choona chimakhala ndi maimvaimva, koma ndi *kwambiri* kuposa maimvaimva. Pali zolakwika ziwiri zokhudzana ndi maimvaimva pa kulambira zimene zikhoza kutisokeretsa.

1. **Kulakwitsa kukana maimvaimva mu kulambira.**

Olambira ena amakaniza maimvaimva mu kulambira. Amaona kulambira monga kukumana ndi Mulungu kwa maganizo; amalephera kuzindikira gawo la maimvaimva pa kukumana ndi Mulungu. Kulambira koona kumayankhula ku maimvaimva. Utumiki wathu wa kulambira uvomereze olambira mmwayi wa kuonetsera kuyankhapo kwawo kwa maimvaimva ku vumbulutso la Mulungu la Iye mwini.

"Kuyimba ndi njira imene anthu a Mulungu amagwirira Mawu ake ndi ku khazikitsa maimvaimva awo ndi zokonda zawo ndi za Mulungu."

Zatengedwa kuchokera kwa Jonathan Leeman

2. **Kulakwika kutsindika maimvaimva mu kulambira.**

Choopsa chosiyana ndi kulakwitsa koyankhula ku maimvaimva mu kulambira pamene kukana maganizo kumaononga 1 Akorinto 14:15; "Tsono pamenepa n'kutani? Ndidzapemphera ndi mzimu wanga, komanso ndidzapemphera ndi nzeru zanga. Ndidzayimba ndi mzimu wanga, komanso ndidzayimba ndi nzeru zanga." Maganizo alionse a kulambira akhoza kugwa ku yesero ili: uthenga umene ndi osakhulupirika ku ndime ya malemba; nyimbo zotakasa maimvaimva zimene zimalephera kuyankhula choonadi cha Baibulo; kulambira kumene kumasokoneza maimvaimva a wolambira. Kulambira kumene kumayankhula ku maimvaimva okha sikulambira koona.

Kupembedza Koona: Kupembedza mu Mzimu ndi mu Choonadi

Chitsanzo cha Baibulo cha kulambira chimalemekeza kufunikira kwa maimvaimva pamene chikusanthula mosamala choonadi cha zimene timalalikira ndikuyimba. Pakuti mayimbidwe ndi gawo la maimvaimva, tikuyenera kukhala osamala maka pa kusanthula

choonadi chimene timayimba. Komabe, pakugwiritsa ntchito bwino, mayimbidwe akhoza kukhala a mphamvu pa kufotokozera choonadi chimene chimalankhula ku maganizo ndi maimvaimva omwe.

John Wesley amaika mtima pa maimvaimva pa kupembedza. Anafotokoza za mpingo wina kukhala "Wakufa ngati miyala – wa chete kwa thunthu, wosakhudzika kwa thunthu." Amakhulupirira kuti kukumana ndi choonadi kulimbikitse kuyankhapo kwa maimvaimva. Pa nthawi yomweyo, anachita changu kutsutsa kuonetsera maimvaimva amene angathe kuononga kulambira koona.

Wesley anachenjeza kupyolera muyeso; kukana maimvaimva kapena kuwavomereza kutilamulira. "Kodi pali kufunikira kwa kuthamangira kwathu mukupyola muyeso kapena wina? Ife tisayende pakati ndi kusunga mtunda waukulu wa mzimu wa zolakwika ndi changu osaletsa mphatso ya Mulungu ndi kutaya mwai waukulu wa ana ake?"[93] Ichi ndi chitsanzo chabwino kwa ife lero: kulemekeza kufunikira kwa maimvaimva mu kulambira, pamene mukupewa kupyola muyeso umene umaononga chindunji chathu pa Mulungu ndi choonadi chake.

Maimvaimva ndi Choonadi: Zokumana nazo za Mkhristu Mmodzi[94]

"Mwa chilengedwe, ine ndine munthu wa tcheru ku maimvaimva. Mayimbidwe akhoza kukhala ndi mphamvu yaikulu pa maimvaimva anga. Ndinaphunzira phunziro zaka zochepa zapitazo za kuika chikhulupiriro chachikulu mu machitachita a maimvaimva anga.

"Pamene ndimamvetsera ku nyimbo ina ya mawu a nthetemya, ndinasunthika kwambiri. Pamene nyimbo imafika pa kusintha mlingo, ndinapezeka ndikulira. Pakufika pamapeto pa nyimbo, ndinamva ngati ndinakhala nditakumana ndi kukumana ndi za uzimu mwakuya.

"Komabe, pamene ndinamvetsera kachiwiri, ndinazindikira chinthu china chodabwitsa: nyimbo imeneyi si inali ya kupembedza Mulungu wa kumwamba. Nyimbo imeneyi imayimba matamando kwa mulungu wa kulambira chabodza. Mawu ake anali a chiphunzitso chonyenga.

"Tsiku limenelo ndinaphunzira kuti maimvaimva akhoza kupusitsidwa makamaka ndi mayimbidwe. Izi sizikutanthauza kuti maimvaimva onse oyankhapo pa mayimbidwe ndi oipa, koma zikutanthauza kuti ndiyenera kusanthula mawu a nyimbo. 'Ndikuyenera kuyesa mizimu' kutsimikizira kuti ikuchokera kwa Mulungu."

---

93 John Wesley, *Mauthenga a John Wesley*, "The Witness of the Spirit."

94 Kalata kuchokera kwa Dr. Andrew Graham. May 29, 2014.

FUFUZANI

Kodi kulambira kwanu kumayankhula ndi maganizo anu komanso maimvaimva anu? Kodi mukusamalitsa kuunika zimene mukuyimba ndi kuphunzitsa kuonetsetsa ndi yokhulupirika ku malemba?

ZOOPSA ZA KULAMBIRA: KUCHEPSA KULAMBIRA

Phunziro ili linayamba ndi chenjezo la Warren Wiesbe kutsutsana ndi kuchita kulambira nthawi zonse.[95] Anachenjeza kuti timachepsa kulambira pamene tikufunafuna zosangalatsa kuposa Mulungu mu mapemphero athu. "Mipingo inakagwiritsa ntchito liwu *kulambira* koma tanthauzo lake linasintha. Mowirikiza *kulambira* ndi liwu limene anthu amagwiritsa ntchito kupereka ulemu wa kulambira ku zonse zimene akonzera mpingo kuti uchite, kaya Mulungu ndiye chindunji cha msonkhano kapena ayi." Kodi izi zimachitika motani?

Ticoka m'malo Opatulika kupita m'malo a Zitsudzo

Kulambira kukhoza kuchitikira kulikonse. Akhristu amalambira mu mapanga pamene akubisala kwa owazunza kapena mmbami mwa moto nthawi ya msonkhano wa mpingo. Akhristu apembedza mmakomo apadera kapena mu nyumba zakale. Akhristu amalambira akugona mu chipatala, kuuluka mu ndege, kapena pa kugwira ntchito. Chipembedzo chingathe uchitikira paliponse, koma kulambira pamodzi kumachitika mnyumba ya mtundu wina wake kwambiri. "Misonkhano ya mpingo ikuyenera kukumana kwina kwake, ndipo 'malo amenewo' asanduke mpingo kapena malo a zisudzo."

Kodi kusiyana kwake ndi kuti? Mpingo "ndi malo amene anthu amakuma kupembedza ndi kulemekeza Ambuye." Malo a zisudzo ndi malo kumene anthu amakakumana kukaonera zochitika. Kodi nyumba ya mpingo wanu ndi ya zisudzo kapena mpingo?

Timasuntha Kuchokera pa Mpingo Kufika pa Gulu Loonerera

Mpingo wolambira umasonkhana kudzalambira Yesu Khristu ndi kulemekeza Iye. Gulu limasonkhana kuti likaone ndi kumvetsera zochitika." Mpingo umakhala ndi otenga mbali; pamena gulu limakhala ndi oonerera. Kodi mukutsogolera mpingo kapena gulu?

---

95 Malemba otengera muchigawo ichi achokera kwa Warren Wiersbe, *Real Worship* (Grand Rapids: Baker Books, 2000), 169-174.

Timasuntha Kuchokera pa Utumiki Kupita pa Kuchita

"Choyambirira timatumikira **kuonetsera** Choonadi cha Mulungu; timachita kuti **tikondweretse** ndi kuthekera kwathu. Mtumiki amadziwa kuti Mulungu akuona ndipo kuvomereza kwake ndiye kofunika koposa zonse; Wazisudzo amafuna kuomberedwa mu manja ndi gulu." Utumiki ukhoza kusanduka zisudzo mu njira zambiri zosiyanasiyana: Woyimba amene amachita chifukwa cha kusangalatsa omvera, gulu la matamando limene limafuna machitidwe ena a maimvaimva, kapena mlaliki amene amayesa ulaliki wake ndi machitidwe a anthu. Kodi mukutumikira kapena kuchita zisudzo?

POMALIZA: UMBONI WA MTUMWI — AROMA 14 MU NTCHITO

"Ndinaphunzira phunziro la bwino la kuweruza ena chifukwa cha mtundu wa kulambira kwawo pamene ndinachita nawo maphunziro atsogoleri ndi mnzanga wa utumwi ndi abusa asanu ndi atatu a chiFilipino.[96]

"Tinalowa malo a msonkhano waukulu ndipo tinapeza pokhala pamwamba mmalo otsika mtengo. Akanema akulu ndi mikuza mawu zinakwezedwa kudenga. Mtsogoleri wa kulambira mzimayi wa chiFilipino othandizidwa ndi gulu la matamando. Amaomba mu manja ndi kutsogolera gulu lokondwera ku 'Inde, Ambuye, Inde!' Inali ya mphamvu kwambiri monga mmene ndimakondera.

"Mayimbidwe obwereza-bwereza, kuyimba kofuwula ndi kuyendetsa thupi kunandikhudza kwambiri. Tinali titalimbikitsa abusa athu a chiFilipino kukhala atsogoleri oyera, ndipo tsopano timawapititsa ku mtundu uwu wa chipembedzo! Mmodzi wa abusa a chiFilipino, mtsogoleri wa uzimu kwambiri, anaima pamenepo mutu wake utawerama. Amapemphera mwakachetechete osatenga nawo mbali mu mapemphero.

"Ndinavutika, 'Kodi tichite chiyani?' Kenako, ndinaona mtsogoleri yemweyu akuombera mu manja ndi kuyimba ndi mtima wake onse. Nkhope yake imanyezimira, ndipo amaoneka kuti wazama mu kupembedza.

"Madzulo amenewo, tinagawana zimene tinaphunzira zokhudzana ndi utsogoleri ku msonkhano. Pa nthawi ya kutembenuka, ndinafunsa mtsogoleri wa chiFilipino ameneyu kuti chinachitika ndi chiyani kuti asinthe machitidwe ake. 'Kodi bwanji munachoka pa kusatenga mbali kufika kuyamba kukondwera ndi kupembedza mwadzidzidzi ndi kukondwera ndi mayimbidwe?

"Yankho lake linali la mphamvu. 'Ndinasokonezeka ndi mayimbidwe. Koma pamene ndimapemphera, Mulungu anandionetsera mtsogoleri wa chipembedzo ndipo anthu mu msonkhano amapembedza Mulungun di mitima yawo yonse. Amapereka kwa Mulungu

96 Umboni kuchokera kwa Rev, Black, mtumwi wakale ku Filipino.

zabwino zawo kulingana ndi zimene amadziwa. Ambuye anati, "Kodi mungawasiye ndi Ine? Kodi mungandipatse kupembedza kwawo popanda kuweruza ena?"'

"Mbusa ameneyu anayamba kupembedza Mulungu ndi mtima wake onse monga mmene amachitira osati kuweruza ena amene anamuzungulira. Kodi izi zinasintha machitidwe ake a kupembedza? Ayi; Atabwerera ku mpingo kwawo, sanayesere mtundu wa chipembedzo umene anaona kumapeto kwa sabata kuja.

"Monga mtsogoleri mu mipingo mwathu, munthu ameneyu amalimbikitsa kwambiri abusa anzake kuti avomere ufulu wa kupembedza mosaononga mpingo. Analimbikitsa abusa anzake kuti akhazikike moyenera mfundo ziwiri izi:

1. Mosamala tsatirani mfundo za Baibulo za kulambira mu mpingo wanu.
2. Pewani kuweruza mitundu ya kulambira mu mpingo wanu."

KUBWEREZA KUONANSO PHUNZIRO 9

1. Chipembedzo ndi chikhalidwe

   - Pa kusanthula mitundu ya chipembedzo, tisasokoneze chikhalidwe ndi malemba.
   - Pamene chikhalidwe chathu chikutsutsana ndi malemba, tikuyenera tidzipereke ku malamulo a amlemba osati ziyembekezo za chikhalidwe.
   - Kuti tifikire dziko ndi uhenga wabwino, tikuyenera tifunse mmene kupembedza kwathukukhoza kulankhulira mwa mphamvu ku chikhalidwe chathu.

2. Mafunso atatu amatithandiza ubale pakati pa mpingo wa pa malo ndi chikhalidwe chozungulira:

   - ***Ndi ndani amene ali pano?*** Amayang'ana mpingo umene ndi gawo la mpingo.
   - ***Ndi ndani amene analipo?*** Kuyang'ana pa cholowa cha mpingo.
   - ***Ndi ndani amene akufunika kukhala pano?*** Kuyang'ana padera kumene tayitanidwa kukafikira.

3. Chifukwa mayimbidwe ndi chionetsero cha chikhalidwe chathu, mipingo isankhe mayimbidwe amene ndi okhulupirika ku Baibulo komanso osamalitsa chikhalidwe.

4. Ngati kuomba mu manja ndi gawo la kupembedza, tikuyenera kufunsa, "Kodi kuomba mu manja ndi koyenera pa nyimbo imeneyi kapena komanso pa nthawi imeneyi ya chipembedzo?"

5. Pa kuomba mu manja kuyankhapo pa nyimbo, tidzifunse, "Kodi komba mu manja kwanga kukulimbikitsika ndi matamando kwa Mulungu kapena ndi oyimba?"

6. Ngati tikusunga ana ndi achinyamata mu mapemphero a akulu, tikonzekere chipembedzo chimene chidzalankhula ndi onse.

7. Ngati timakhala ndi mapemhero osiyana a ana ndi achinyamata, tionetsetse kuti mapemphero alia a chipembedzo osati kusangalatsa.

8. Tisatsindike kupyolera muyesokapena kukaniza maimvaimva mu chipembedzo.

NTCHITO YA PHUNZIRO 9

1. Phunziro limeneli linali ndi mafunso a “fufuzani” angapo. Lembani mayankho pa tsamba limodzi pa funso limodzi mwa mafunso amenewa. Yankho lanu likhale ndi magawo awiri:

    - Kusanthula kwa zimene mumachita pano mu chipembedzo.
    - Kuvomereza kwa kusinthakumene kudzapangitsachipembedzo chanu kugwirizana ndi chikhalidweposachoka ku mfundo za Baibulo pa chipembedzo.

2. Ku mayambiriro kwa phunziro lotsatira, mudzalemba mayeso ochokera pa phunziro limeneli. Werengani mafunso a mayeso mosamala pokonzekera.

MAYESO A PHUNZIRO 9

1. Kodi tiyenera kuchita motani ku machitidwe opembedza amene sagwirizana ndi zofuna za chikhalidwe chathu koma satsutsana ndi mfundo za Baibulo?

2. Kodi tiyenera kuchita motani ku machitidwe a kulambira amene ali ololedwa mu chikhalidwe chathu, koma amatsutsana ndi malemba?

3. Kodi ndi mafunso atatu otani amene tiyenera kufunsa kuti timvetsetse ubale wa pakati pa kulambira kwa mpingo wathu ndi chikhalidwe chozungulira?

4. Kuchokera pa Aroma 14, tchulani mfundo zitatu zogwirizana ndi kulambira.

5. Tchulani malingaliro atatu okhudza chipembedzo chopatsira m'badwo wina.

6. Tchulani zolakwika ziwiri zokhudzana ndi maimvaimva pa chipembedzo.

7. Lembani 1 Akorinto 14:15-17 kuchokera pakuloweza.

PHUNZIRO 10

MOYO WA CHIKHALIDWE CHA KULAMBIRA

ZOLINGA ZA PHUNZIRO

1. Kuzindikira ubale wa pakati pa kulambira kwa gulu ndi moyo wa chikhalidwe cha kulambira.
2. Kudziwa kuti moyo wa chikhalidwe cha kulambira umasintha zochitika za munthu.
3. Kufuna kukhala ku ulemelero wa Mulungu.
4. Kukhala odzipereka ku moyo wa chikhalidwe cha kulambira chimene chinaphunzitsidwa pa Aroma 12:2.
5. Kufotokoza maziko a Baibulo a kulambira.

KUKONZEKERA PHUNZIRO ILI

Lowezani 1 Akorinto 10:31.

CHIYAMBI

Muchaka chomwecho, mtundu wa ku Africa ukuoneka pa mindandanda iwiri: “Chiwerengero cha Akhristu ochuluka mu Africa” komanso “Mtundu wa ziphuphu zochuluka mu Africa.”

M’busa wina wa mpingo wa ukulu ku Asia akuyimbidwa mulandu wozembetsa ma miliyoni a ma dollar.

Mtsogoleri wina wa mpingo waukulu watula pansi udindo atavomereza kusakhupirika pa banja.

Kodi chavuta ndi chiyani? Pali zinthu zambiri zokhudzana ndi izi, koma chinthu chimodzi ndichofanana kwa onse: Kulambira kwa pa Sabata sikukhudza moyo wa tsiku la pa Mande. Tsiku lasabata ndi tsiku limene timatengedwa kuti ndi "lolambira" – kukhudzika ndi la chidwi. Tsiku la pa Mande limatengedwa kuti ndi tsiku "la moyo weniweni" – ntchito zosakhala bwino komanso kukonda zodzisangalatsa wekha. Kwa anthu ambiri, zochitika za kulambira sizithera ku moyo wosinthika.

» Kambiranani mmene kulambira kumakhudzira moyo wanu wa tsiku ndi tsiku. Kodi zochita zanu zimayenda mosiyana chifukwa cha kulambira kwanu? Kodi ubale wa banja lanu ndi osiyana motani chifukwa cholambira? Nanga chikhalidwe chanu? Ndale zanu? Kayendetsedwe ka chuma chanu? Kodi muli ndi chikhalidwe cha moyo wolambira?

KULAMBIRA: KUPOSA TSIKU LA SABATA

Vuto limene lakambidwa pa chiyambi cha phunziroli silachilendo. Amosi anayankhula ndi anthu amene anabweretsa nsembe ndi kutsatira miyambo ya ku Kachisi, koma analephera kukhala moyo wa umulungu (Amosi 5:21-24). Yeremiya analalikira kwa anthu amene amakuwa, "Kachisi, Kachisi," koma sanadziwe zoona za kupezeka kwa Mulungu (Yeremiya 7:4). Yesu ananena za onse amene anatsata bwino malamulo, amene anapereka chakhumi chochepetsetsa, amene anali okhulupirika ku pemphero, otsata tsiku la Sabata, ndi miyambo ina yolambira, koma amene mitima yawo siyinali yoyera (Mateyu 23:23). Anthu awa anadzinena kuti ndiwolambira, koma kulambira kwawo kunali kwabodza. Kulambira koona kumakhudza moyo onse.

Paulo analemba kwa wokhulupirira amene anakumana ndi nkhani ya nyama imene inaperekedwa ku mafano. Atayankhulapo pa vutoli, Paulo anamalizira ndi kuti, "N'chifukwa chake chilichonse mungadye kapena kumwa, kapena chimene mungachite, chitani zonse ku ulemerero wa Mulungu" (1 Akorinto 10:31). Pamene Paulo amanena za nyama yoperekedwa ku mafano, fundoyi ikukhudza madera onse a moyo. Ngati timalambira moona, miyoyo yathu ya tsiku ndi tsiku idzakhalidwa ku ulemerero wa Mulungu.

"Mtsogoleri wachipembedzo akhale munthu amene aike chitsanzo za kulambira mu magawo onse a moyo; amene adzafunafuna Mulungu ndi chilichonse; amene adzatsogolera mpingo mu chikhalidwe chonse chachipembedzo."

Zatengedwa kwa Stephen Miller

Tanthauzo limodzi la kulambira ndi "...zonse zimene ife tingachitire chimene tili kwa Mulungu."[97] Tanthauzo ili likuonetsa kuti kulambira kudzakhudza zochitika zathu zonse pa za moyo. Pali mfundo ziwiri zimene zikhoza kuyikidwa mofanana potanthauzira mawu a kulambira.

Kulambira Kwaguluu: Kulambira kwa Tsiku la Sabata

Kulambira kwakukulu kumanena za kukumana kwa thupi lonse la tchalitchi. Mkumano uwu ukhoza kuchitikira mu nyumba ya tchalitchi, mnyumba, kapena chikonzero china. Pochitikira sipofunikira kwambiri, koma nthawi yoyikidwa pa nkumano wolambira waukulu ndizo zofunikira. Akhristu amapatsidwa mwayi ndi udindo wosokhana kolambira kwakukulu (Ahebri 10:25).

Moyo wa Chikhalidwe cha Kulambira: Kulambira mu Moyo Wonse

Mu munda wa Edeni, munakamufunsa Adamu ndi Eva, "Kodi mumalambira nthawi yanji?" akanayankha, "Timalambira nthawi iliyonse, Moyo wathu wonse ndi kulambira." Uku ndi kulambira ngati mwachikhalidwe.

Kulambira ndi mkumano waukulu wa okhulupirira ndi moyo wokhala ndi ulemelero wa Mulungu. Mu zaka chikwi za chiwiri, Bishopu Iraeneus wa ku Lyons anati, "Ulemelero wa Mulungu ndi munthu amene ali ndi wa moyo wonse." Si chinthu chokhazikika cha umunthu; ndi chinthu chokhazikika cha Mulungu. Uku ndiko kulambira kwenikweni.

Ngati Akhristu timapereka zonse za moyo wathu, kwa Mulungu. Kulambira sikukhala kwa tsiku la Sabata lokha ayi. Ntchito zathu, masewera athu, ndi zonse zimene timachita, timachitira ulemelero wa Mulungu. Aroma 12:1 ikuonetsa kuti kulambira kumakhudza kudzipereka kwa matupi athu ngati nsembe; iyi ndiyo ntchito yathu ya uzimu. Maganizo a zolambira za mu Baibulo sangakhale oti kulambira kukhale kokumana pa Sabata basi; komatu ndikudzipereka kwa moyo wathu onse kwa Mulungu.

"Nsembe ya moyo wathu kuntchito ya Mulungu tsiku ndi tsiku ndimaitanidwe a moyo wathu wonse. Kulambira kwa mmawa wa tsiku la Mulungu ndikupitiriza za maitanidwe amenewo."

Barry Liesch

Maganizo a kulambira mu Baibulo amakhala ndi kulambira kwa gulu komanso moyo wa tsiku ndi tsiku. Mbali zonse ziwiri ndizofunika. Ngati tiiwala kuti kulambira ndikokhudza tsiku lililonse, tikhoza kupita ku malo olambira osaona

97 Warren Wiersbe, *Real Worship*. (Grand Rapids: Baker Books, 2000), 21.

chilichonse chotikhudza pa moyo wathu wonse. Izi zimatitsogolera kukalambira nawo ndi gulu pamene takanika kukhala omvera kwa Mulungu tsiku lililonse.

Komabe, titatsimikiza "kulambira ndi kwa moyo wonse," timayiwala kufunikira kwa nthawi yoyikidwa pambali kuti tiike mtima polambira. Kukhala nawo polambira pa gulu kumakumbutsa ife za kutumikira kwa Mulungu pa moyo wathu.

Mfundo udindo ikuoneka pa za chakhumi ndi Sabata. Udindo wa Mkhristu utanthauza kuti ndalama zathu zonse ndi za Mulungu; chikhulupiliro chathu mu mfundo imeneyi chimaonekera ndi chakhumi chathu. Mmene Mkhristu amaonera za nthawi zitanthauza kuti moyo wake uli wa Mulungu; timaonetsera kuti tikadzipereka kwa tsiku limodzi pa sabata kulambira kenako ndikupuma. Mwanjira yomweyo, zonse zochitika za moyo wathu ndi mbali imodzi yolambira; timaonetsera zimenezi posonkhana ndi anzathu okhulupirira polambira mwapagulu.

Bob Kauflin anaonetsa ubale wa pakati pa kulambira pagulu ndi kulambira mwa chikhalidwe:

> Tsiku la Sabata likhoza kukhala tsiku lapamwamba la sabata yatha, komatu sikuti ndi zokhazo. Mkatikati mwa sabata, timakhala moyo wolambira pamene tikonda banja lathu, tikana mayesero, tiyimira molimba mtima, anthu amene ali ovutika, kulimbana ndi zausatana, ndikutchula za uthenga wabwino. Mu zinthu zonse izi ndife **wolambira a tchalitchi obalalikana**.
>
> Koma timatopa mu nkhondo zathu zolimbana ndi dziko, thupi lathu, ndi woipayo ndipo timafunika kulimbikitsidwa ndi Mau a Mulungu, ndi chisamaliro cha ena woyera. Tikufuna kupanga ubale ndi iwo amene Mulungu wawalumikizitsa ndi ife kudzera mu mwazi wa mwana wake. Ndiye timakumana kuti tikhale **wolambira a tchalitchi okhala pamodzi**.[98]

KULAMBIRA: KUKHALA KU ULEMELERO WA MULUNGU

Kulambira Kumaonetsa Kufunikira Kwathu

Tinalengedwa kuti tilambire. Tonse timalambira winawake kapena chinachake. Timalambira chimene chili chofunikira kwa ife. Kulambira kumati, "ichi ndi chimene chili choyamba m'moyo wanga."

Anthu ambiri amalambira ndalama, zochita zawo, ubale, kapena zokonda zawo. Zinthu izi zimayambirira kuchitika mmoyo wawo. Kodi mumadziwa bwanji za chimene mukulambira? Taonani za moyo wanu, kodi ndi chiyani chimene chimatenga gawo lalikulu, nthawi kapena

98 Bob Kauflin, *Worship Matters* (Wheaton: Crossway Books, 2008), 210.

ndalama? Izo ndi zimene mwasankha kuti zikhale zofunika kwa inu; zimenezo ndizo mukulambira.[99]

Mulungu yekha ndiye woyenera kulambira; zina zonse zikubwera pambuyo. Chikhalidwe cholambira chimayika Mulungu patsogolo pa zonse. Wolambira woonadi amayika Mulungu pa mpando wolamula mmoyo wawo; Iye ali ndi mtengo wapamwamba kuposa zonse. Izi zitanthauza kuti kwa wolambira woonadi, moyo wawo wonse ukhala ku ulemelero wa Mulungu.

Kulambira koonadi Kumasintha za Chikhalidwe chathu

Mu Yesaya 6, tikuona kuti kulambira koonadi kukusinthika. Kulambira sikuonetsa makhalidwe athu okha basi, kumasinthanso makhalidwe athu.

Kulambira, kwa Mulungu kapena kwa mafano, kumasintha za mmene ife tili. Masalimo 115:8 akuonetsa kuti kulambira mafano kumatisintha kukhala woyipa. "Anthu amene amapanga mafanowo adzafanana nawo, chimodzimodzinso onse amene amadalira mafanowo." Wopembedza mafano amakhala ngati mafano. Iwo wopembedza ndalama amakhala adyera lochuluka; amene amatamanda zosangalatsa moyo amakhala akapolo a zosangalatsazo; amene amalambira kutchuka amakhala odzikonda. Timakhala chimene tilambira.

"Aliyense ali ndi guwa. Guwa lililonse lili ndi mpando waufumu. Nanga kodi mungadziwe bwanji chimene mupembedza? Nzosavuta: tsatirani njira ya nthawi yanu, chikondi chanu, mphamvu zanu, ndalama zanu, ndi za mbali yomwe muli. Komaliza kwa kanjira aka mupeza mpando waufumu, ndipo pa chilichonse, kapena aliyense amene mupeze pa mpandopo ndi chimene chili chinthu cha mtengo wapatali kwa inu, chimene chili pa mpandopo ndi chimene mudzapembedza."

Louie Giglio

Chomwecho, amene alambira Mulungu amakhalanso mofanana ngati Iye. "Ife tonse amene tili ndi nkhope zosaphimba, timaonetsera ulemelero wa Ambuye, tikusinthika kufanana ndi ulemelero wake umene ukunka nuchulukirachulukira" (2 Akorinto 3:18).

Kulambira sichinthu choti timangopanga; kulambira kumatipangira chinachake.

99 Zachokera kwa Louie Giglio, *The Air I Breathe: Worship as a Way of Life*. (Sisters, OR: Multnomah Publishers, 2003).

Pamene tilambira chikhalidwe chathu chimasintha.ngati wolambira, tiyenera kufunsa, "Kodi kulambira kukusintha moyo wanga?"

Kukhala ku Ulemelero wa Mulungu Kumakhudza zonse za Moyo

Kulambira ngati chikhalidwe kutanthauza kuti moyo wonse ukhala ku ulemelero wa Mulungu. Akhristu ambiri amagawa nthawi yawo ku zinthu ziwiri zosalumikizana: tsiku la Mulungu loyera ndi masiku ena a musabata (Lolemba mpaka Loweluka). Amakhala ngati a Khristu a "tsiku la Mulungu" Amakhala nao kumapemphero ku tchalitchi ndikunena kuti iwo ndi a Khristu okhulupirira, koma kulambira kwa tsiku la Mulungu sikukhudzana ndi zochitika za tsiku Lolemba, tsiku Lachitatu ndi lokhala ndi a pabanja, kapena tsiku Loweruka lachisangalalo.

Mawu awa *zamitundu* akunena za moyo wa mdziko. Mkhristu pa tsiku Lolemba akuyenera kuonetsa zimene zamukhudza zomwe anaphunzira pa Sabata ku tchalitchi. Pomaliza pa mwambo wa mapemphero, tizidzifunsa, "Kodi mawa ndipange chiyani kuti ulaliki wa lero ugwire ntchito?" Uwu ndi moyo womwe ukukhalidwa ku ulemelero wa Mulungu.

Kodi kukhala ku Ulemelero wa Mulungu kumaoneka motani?

Kukhala ku ulemelero wa Mulungu kutanthauza kuti moyo wathu ukuyenda ndi chikondi cha Mulungu. Zitanthauza kuti kukonda Mulungu mpaka kufika pakuti chimwemwe chathu chimusangalatsa Iye. Munthu wina anati kukonda munthu ndi kukhala wotangwanika naye. "Uli mu chikondi ndi winawake (kapena chinthu) kuti mpaka umaganizira nthawi imene sukuganiza za china chili chonse."

Mwanjira yomweyi, Louie Giglio anaganiza kuti "tikudziwa chimene chili choposa zonse mu mzimu wathu pa zimene zimatuluka pakamwa pathu."[100] Timalakhula za zinthu zomwe zili zofunika kwambiri kwa ife.

Zikhoza kuoneka kuti ndizophweka, koma taganizirani. Kodi munthu amene amakonda ndalama amakamba za chiyani? Ndalama. Amaika ulemelero pa ndalama. Kodi munthu wokonda za masewera amakamba za chiyani? Za masewera. Amakweza mwaulemelero za magulu a masewera amene akuwakonda.

Kodi izi zitanthauza kuti Mkhristu azingokamba za Baibulo nthawi zonse? Ayi; zikutanthauza kuti zonse zimene timakamba zikhale zokweza ulemelero wa Mulungu. Pamene tikufuna kupanga chiganizo chokhuza za malonda, sitingathe kunena kwa anzathu ogwira nawo ntchito kuti, "Chiganizo ichi chilemekeze Mulungu," koma ulemelero wa Mulungu udzakhudza maganizo athu. Pamene tifuna kulangiza mwana, sitingayambe ndikunenena kuti, "Mwana wanga, ndikufuna kuti kukwapula uku kutamandire Mulungu," koma

100 Louie Giglio, "Psalm 16" in Matt Redman and Friends, Inside, Out Worship (Ventura: Regal Books, 2005), 78.

tidzifunse tokha, “Kodi kulanga, kumusangalatsa Mulungu kapena ndingofuna kuchotsa mkwiyo wanga? Kodi umu ndi mmene Atate wanga wakumwamba angandilangire ine?”

Monga akhristu, timapanga ziganizo mu kuwala kwa Ulemelero wa Mulungu. Kulambira ngati chikhalidwe chitanthauza kuti Mulungu ndi Ulemelero wake zili pakati pa zonse zimene timachita.

Muphunziro loyambirira, tinaona kuti kupatula za chisomo, kulambira kwa gulu kumakhala kokhazikika, kumene timafunsa, “Kodi timalambira munjira yotani imene imatipezera chisomo cha Mulungu?” Munjira yomweyo, kupatula chisomo, chikhalidwe cha kulambira chimakhala chinthu chokhazikika cholemetsa, chimene timafunsa, “Kodi bwanji chiganizo ichi chitakhala kuti sichabwino pa njira yolambira Mulungu? Kodi nditalakwitsa, Mulungu akhoza kukwiya?”

Mongosiyana ndi kulambira kokhazikika, kulambira mkuwala kwa chisomo cha Mulungu chimakhala mwayi wapamwamba. Kulambira kwa pa gulu mkuwala kwa chisomo cha Mulungu ndi mwayi woti tisangalale za kuti Mulungu ndi ndani ndi zimene wachita. Munjira yomweyo, chikhalidwe cholambira (ukakhala mkuunika kwa chisomo cha Mulungu) ndi mwayi wolambira Mulungu pa moyo wa tsiku lililonse.

Zochitika za tsiku la Lolemba, zisatipangitse kusiya kutsata malamulo a Mulungu. Ndi chinthu cha mwayi kulemekeza Mulungu ndi chikhalidwe chimene sichimasintha ndi machitidwe ake. Kulanga mwana sichinthu chimene chingatipangitse kusasangalatsa Mulungu; ndi chinthu cha mwayi kuti tithe kukonzanso khalidwe lokonda Mulungu kwa mwana wanu. Chisomo chimasandulitsa moyo wanu wa chipembedzo.

CHIKHALIDWE CHOLAMBIRA: CHITSANZO CHA MU BAIBULO

Mu Aroma 12:1, Mkhristu akuyitanidwa kudzipereka yekha nsembe yamoyo, yoyera ndi yovomerezeka kwa Mulungu. Uku ndikulambira kwathu kwa uzimu. Aroma 12:2 ikuonetsa mmene nsembe iyi ingaperekedwere. Malemba awa ndiofunikira pofuna kuzindikira za chikhalidwe cholambira.

Pambuyo pa ndime khumi ndi imodzi mmene Paulo amaika maziko a moyo wa chikhristu, akufika ku ndimen yofunika kuchitapo kanthu. Chifukwa chakuti talungamitsidwa

mwachisomo (Aroma 1-11), tikuyenera kukhala mwanjira ina yake (Aroma 12-16) Ndime izi zimapereka chitsanzo cha moyo chikhalidwe cha kulambira.

Mbali Yoyipa ya Chikhalidwe cha Kulambira

Paulo akuyamba ndi kulamula kotsutsa: "Musafanizidwenso ndi makhalidwe adziko lino." Tisakhale padziko lapansi kufanizira nalo. Sitingagonje padziko komanso ku ufumu wakumwamba; sitingalambire Mulungu komanso mzimu wa masiku ano.

J.B Philips anamasulira malangizo a Paulo, "Musalore kufinyidwa ndi dziko lapansi ngati dongo." Pamene dongo laumbidwa, limatenga maonekedwe a chimene mukufuna kuumba. Dziko lapansi likufuna lifinye akhristu kukhala mumaonekedwe ake. Dziko lapansi likufuna litikakamize kugonjera ku zofuna zake. M'malo mwake, tikuyenera kukhala ndi chikhalidwe cholambira, kuti tikane zochitika za mdziko lapansi.

Mayesero awa ndi owopsa chifukwa tikhoza kugwamo tisanazindikire za kuumba kwake. Nsomba ya m'madzi siganiza, "Awa ndi madzi." Umu ndi mmene nsombayi imakhala. Nyongolotsi imene imayenda mu matope siganiza, "Awa ndi matope" Umu ndi mmene nyongotsi imakhala. Ngati sitikhala tcheru, Mkhristu wokhala pa dziko lakugwa sangaganize, "Ili ndi dziko lakugwa." Likhoza kukhala dziko limene tikukhala.

Kodi ndi chifukwa chiyani kupemphera kwagulu kuli kofunikira. Wolemba wachiyuda anachenjeza kuti asanyalanyaze zokumana pamodzi. Chifukwa? Chifukwa umu ndi mmene timakwaniritsira malamulo ena:

- "Tsono tiyeni tiyandikire kwa Mulungu ndi mtima woona ndi wodzaza ndi chikhulupiriro. Popeza mitima yathu yayeretsedwa, ndi yopanda chikumbumtima chotitsutsa, ndiponso matupi athu asambitsidwa ndi madzi woyera" (Ahebri 10:22).
- "Tiyeni tigwiritsitse mosagwedezeka zimene timaziyembekezera ndi kuzivomereza, pakuti amene anatilonjezayo ndi wokhulupirika" (Ahebri 10:23).
- "Tiziganizira mmene tingalimbikitsirane wina ndi mnzake pokondana ndi kuchita ntchito zabwino" (Ahebri 10:24).

Polambira tikukumbutsidwa kuti ife si apadziko lino. Ku Babulo, anasiyanitsidwa ndi Kachisi, atakanizidwa kulambira pa gulu ndi anthu amtundu wake, Danieli amapemphera katatu patsiku, zenera lake titapenya ku Yerusalemu (Danieli 6:10) Kulambira kunamulimbikitsa Danieli kusatengeka ndi za mdziko la ku Babulo. Pamene amayang'ana ku Yerusalemu, Danieli anakumbutsidwa, "Ine sindine nzika ya ku Babulo. Ine sindilambira Marduk; Ndimatumikira Yehova."[101]

101 Zatengedwa kuchokera kwa Tim Keep, Bible Methodist Missions. Chapel sermon at Hobe Sound Bible College, November 2013.

Chikhalidwe chachipembedzo chitanthauza kukana kufinyidwa ndi zinthu za mdziko. Uku ndikukanitsitsa zinthu za mayesero zamitundu. Uku ndi monga ngati kuonetsetsa za malamulo oyikika. Izi ndi zodutsilira pa za mtundu wa za mavalidwe, malamulo a chikhalidwe, kapena chikhalidwe cha chipembedzo. Zikutanthauza kuonanso zonse zokhudza Ufumu wa Mulungu.

Monga ngati Akhristu, sitingathe kukhala mokwana bwinobwino mu chikhalidwe chomwe chatizungulira. Wophunzira wina ku China, atamaliza kuphunzira za pa phiri, anati, "Ku China nkovuta kukhala mmene Yesu anaphunzitsira." Mphunzitsi anati, "musadabwe, ku America, nkovutanso kukhala monga mmene Yesu anaphunzitsira." Mchikhalidwe chili chonse, chikhalidwe cholambira chimalimbana ndi mzimu wa dziko lapansi.

M'mbali Yabwino ya Chikhalidwe Cholambira

Motsatira chilamulo chotsutsana, Aroma 12 akupitiriza ndi malangizo ake zabwino: "sandulikani pokonzanso maganizo anu."

Kutembenuza kwa zotengera za mdziko lapansi sikukhala kusiyana chabe kapena kutengera za chikhalidwe chanu. Kutembenuza kotengera za mdziko, ndikukhala osandulika mpaka utadziwa za chifuniro cha Mulungu. Akhristu ena atsatira chikhalidwe chosiyana ndi chawo, koma sanasandulike ku chifuniro cha Mulungu. M'malo mwake, asinthanitsa ndi maonekedwe ena a zandale, zochitika pamoyo wa munthu, mavalidwe a chikhalidwe cha pa dziko lapansi. Sanasandulike pokonzanso za moyo wawo.

J.B Phillips anamasulira motere, "Musaole dziko lapanso likufinyeni inu monga mmene lili" (zotsutsana), "komatu muloleni Mulungu akupangeninso kuti maganizo anu onse asinthike" (zabwino). Buku lonse la Aroma likuonetsa mmene moyo wa wosandulika umakhalira.

- Aroma 12: Wokhulupirira wosinthika amagwiritsa ntchito mphatso zake za uzimu kutumikira ena.
- Aroma 13: Wokhulupirira wosinthika amapereka ulemu kwa wolamula.
- Aroma 14: wokhulupirira wosinthika amavomereza kumangidwa kwa okhulupirira ena.

Chikhalidwe cholambira ndi chosiyana ndi machitidwe; kulambira kumasandulitsa za maganizo athu onse. Taganizirani za mmene chikhalidwe cha kulambira chingakhazikitsidwire.

- Kodi dziko la Africa likhoza kuoneka motani Akhristu ochita malonda ndi andale atasandulika pa machitidwe awo pokhudzana ndi ndalama komanso mphamvu za ulamuliro?

- Kodi matchalitchi aku Asia akhoza kuoneka motani ngati atsogoleri ake atasanduka otumikira ndalama za Mulungu?

- Kodi maukwati angaoneke motani ku America ngati Akhristu ataona za kusakhulupirika ndi maso a Mulungu kusiyana ndi maso a ku Hollywood?

Chikhalidwe cha chipembedzo chimasintha maganizo a wokhulupirira; maganizo osinthika amaoneka kusinthika kwa moyo; maganizo osinthika amasinthanso anthu ena. Chikhalidwe cholambira chikhoza kusintha kwambiri dziko lathu.

ZINTHU ZOOPSA POLAMBIRA: KULAMBIRA KOPANDA NAKO KUMVERA

Aneneri anachenjeza za kulambira kosamvera nako. Anthu a nthawi ya Yeremiya anakhulupirira kuti Kachisi adzawateteza iwo ku Babulo. Yeremiya anayankhapo, "Musamakhulupirire mawu anu achinyengo onena kuti, 'Ino ndi Nyumba ya Yehova, Nyumba ya Yehova, Nyumba ya Yehova!'" (Yeremiya 7:4) m'malo mwake.

> **Ngati** mukonzanso za mayendedwe anu ndi zochita zanu;
>
> **Ngati** mupereka chilungamo kwa wina ndi mzake;
>
> **Ngati** simupondereza, apaulendo, opanda atate wao, amasiye kapena kukhetsa mwazi m'malo awa, ndipo ngati muleka kutsatira milungu ina kuti ingakuonongeni;
>
> **Kenako** ndidzakulolani kukhala pa malo awa, mu dziko limene ndinapereka kwa makolo anu mpaka muyaya (Yeremiya 7:5-7).

Anthu a ku Israeli anakhulupirira kuti akhoza kusinthanitsa miyambo ndi kumvera. Aneneri anaphunzitsa kuti miyambo yopanda kumvera ndiyopanda pake.

Mu chikhalidwe china, kumvera kumalowa m'malo mwa miyambo yopemphera. Kumene zopemphera zimapezekako. Nyimbo zimakamba zoonadi. Mawu amawerengedwa ndi kuphunzitsidwa. Mapemphero amachitika. Komabe kulibe za kusamvera ku Mawu a Mulungu. Miyoyo sisinthidwa. Iyi ndi miyambo osati kulambira.

Mu zikhalidwe zina, kumvera kumalowa m'malo mwa kukhudzika. Cholinga cha zochitikazi ndi kupanga maganizo a mtundu wina wake. Nyimbo zimayambitsa maganizo okhudzika. Chiphunzitso chimatsogolera ku mayitanidwe kapena nthawi yodzipereka. Komabe, mwambo wamapemphero siumatsatilidwa ndi moyo omvera komanso kugonja kwa Mulungu. Uku ndi kukhudzika, osati kulambira.

Kulambira kwa mu kachisi kunasangalalidwa ndi pangano la ana Aisraeli ndi Mulungu, ndipo anakumbutsidwa za pangano ndi udindo wawo. Muchipembedzo chakale, kulambira kumakumbukiridwa ku pangano latsopano limene linaperekedwa kudzera ku imfa ya Yesu

ndipo kunakumbutsa Akhristu onse za udindo wawo ku moyo woyera. Kulambira kumene sikumabweretsa kumvera, ndikwachinyengo.

Kulambira koona kumasandulitsa wolambira. Mu phunziro lonse ili, taona kuti anthu amene amalambira moonadi amasinthika moyo wawo. Cholinga cha maphunziro awa sikuti mungodziwa kukhala wodziwa kupanga kapena kutsogolera mwambo wa chipembedzo, komatu kuti mukhale wolambira amene wasandulika ndi kulambira. Kenako mutha kutsogolera kulambira kumene kudzasintha aliyense mu mpingo.

KUMALIZITSA: UMBONI WA M'BUSA

Kodi kulambira koona kumeneku nkokhudzika motani? Tamvani kwa m'busa wa tchalitchi china ku Spain.

"Mu chaka cha 1991, nyengo ya za uzimu pa tchalitchi chathu inatsika kwambiri. Chiwerewere chinakhazikika kwa ena a mu tchalitchi. Akapatsidwa chilango Akhristu akugwawo, tchalitchi chimagawanikana. Kenako, pokhudzika ndi mzimu woyera, wolambira wina watsopano anaganiza kuti tisale kudya ndi kupemphera tsiku lonse la Sabata. Tinapanga izi kenako Mulungu anayamba kutiyendera."

"Patapita masabata angapo, tinayamba mkumano wathu wapachaka. Kugawanika mu Mpingo mbali ina kunatsalirabe. Pamene mlaliki anayamba kuphunzitsa za mawu usiku pa tsiku Lachitatu, anamva nkati mwake kuti Mulungu wamuuza kuti ayimbe, 'Ndinu Wankulu.'

"Pamene anayimba nyimbo iyi, ulemelero wa Mulungu unatsika pa gulu la njala. Ena anachilandira ndi kumutamanda; ena anafunafuna Mulungu pa guwa. Mayi wina amene amayambitsa mikangano ya pa tchalitchi analira mokweza. Anayima kutsogolo kwa gulu la wanthu okwana 400, ndikulapa, 'Ine ndi mayi wosasangalala chifukwa ndinamuchimwira Mulungu ndi tchalitchi chake pobisa chikhululukiro mu mtima mwanga. Ndikupempha Ambuye andikhululukire, ndikupemphanso mpingo undikhululukire.'

"Pamene mawu awa amatuluka pakamwa pake, ena anakhululukirana. Madzulo atsiku limenelo, Mulungu anabwezeretsa mgwirizano pa mpingo wathu. Ngati anthu a Mulungu anadzichepetsa mu pemphero ndi kusala kudya, ndipo ngati anthu antchito a Mulungu anakhala omvera ku utsogoleri wa Mzimu Woyera, tinafika popezeka Mulungu. Machimo anaululidwa; mgwirizano unabwezeretsedwa. Izi ndi zotsatira za kulambira koonadi."[102]

102 Umboni wa m'busa Sidney Grant, Hope International Missions.

KUBWEREZA KUONANSO PHUNZIRO 10

1. Kupemphera kwa gulu kumachitika pa tsiku la Mulungu; chikhalidwe cholambira chimachitika pa moyo wa tsiku lililonse. Zonse zofunika malinga ndi mmene Baibulo likunenera.

2. Kulambira koonadi kumaonetsa chimene chili chofunikira.

3. Kulambira koonadi kumasintha chimene chimakhala chofunikira kwa ife.

4. Chikhalidwe cholambira chikutanthauza kuti kukhala mu ulemelero wa Mulungu. Ichi chitanthauza kuti Mulungu akhala pakatikati pa moyo wonse.

5. Chitsanzo cha mu Baibulo cha za kalambilidwe chikuoneka pa Aroma 12:2. Chikuti

   - Mbali yotsutsa: “Musafanizidwenso ndi makhalidwe adziko lino.”
   - Mbali yabwino: “Sandulikani pokonzanso maganizo anu.”

NTCHITO YA PHUNZIRO 10

1. Lembani pa masamba atatu kapena anayi za nkhani imene mutu wake ndi “Kuphunzira Kulambira.” Kulemba uku kuonetse mmene kulambira kumachokera pa mfundo za mu malemba. Zolembazi zikhale zokhudza za mu Baibulo komanso zochitika.

2. Lalikirani chiphunzitso cha pa za kulambira koonadi malingana ndi Yohane 4:23-24.

3. Kumaliza ntchito ya: Lembani ripoti la tsamba limodzi la mtsogoleri wa kalasi limene likufotokonza za zimene mwaphunzira kuchokera pa “Masiku 30 a Ulendo wa Kulambira.” Simukusowekera kupereka buku lanu.

4. Pa za mayeso anu omaliza, lembani 1 Akorinto 10:31 kuchokera pakuloweza.

MLOZERA A:

NDONDOMEKO ZA KUKONZEKERA MWAMBO WA MAPEMPHERO

MNDANDA WA KULAMBIRA MOZUNGULIRA ZA CHIPHUNZITSO		
CHOLINGA	**ZOCHITIKA POLAMBIRA**	**ZOCHITA ZA SABATA NDI SABATA**
Kulalika za Choonadi	• Nyimbo • Malemba • Uthenga	
Kuyankhako ndi Zoona	• Kuitanidwa • Kupereka • Nyimbo Yotsekera • Mdalitso (Malemba)	

MNDANDNDA WA KULAMBIRA KUTENGERA PA MASALIMO 95		
CHITSANZO CHA MU BAIBULO	**ZOCHITIKA POLAMBIRA**	**ZOCHITA ZA SABA-TA NDI SABATA**
Kulowa ndi Chisangalalo cha Chiyamiko	• Kuyitana pa Kulambira • Nyimbo Za Matamando	
Kupitiriza ndi Kulambira kwa Ulemu	• Nyimbo za Kudzipereka • Pemphero	
Kumvera Mawu a Mulungu	• Kuwerenga Malembo • Uthenga	

MNDANDANDA WA KULAMBIRA KUTENGERA NDI ZOCHITA ZA ANTHU A MULUNGU POLAMBIRA		
KUYENDA	**ZOCHITIKA POLAMBIRA**	**ZOCHITA ZA SABATA NDI SABATA**
Kukumana kwa Anthu a Mulungu	Kutamanda • Kuyitana pa Kulambira • Nyimbo za Matamando Kulapa • Pemphero	
Anthu Mulungu Amva Mawu	• Kuwerenga Malembo • Uthenga	
Anthu a Mulungu Achitepo kanthu pa Mawu	• Nyimbo yoti Tichitepo Kanthu • Pemphero • Kupereka	
Anthu a Mulungu Atumizidwa Kunja	• Nyimbo Yotsekera • Mdalitso (Malemba)	

MNDANDA WA POLAMBIRA KUONETSA ZOLANKHULANA PAKATI PA MULUNGU NDI ANTHU AKE (YESAYA 6)		
ZOCHITA	**ZOCHITIKA POLAMBIRA**	**ZOCHITA ZA SABATA NDI SABATA**
Mulungu Adziulula	• Mayitanidwe Akulambira (kuchokera mu Malemba)	
Anthu Ayankha ndi Kutamanda komanso Kulapa	• Kutamanda: Nyimbo • Pemphero	
Mulungu Ayankhula ndi Anthu Ake	• Kuwerenga Malembo • Uthenga	
Anthu Ayankha Podzipereka	• Nyimbo Yoyitanira • Kupereka	
Mulungu Adzodza Anthu Ake	• Mdalitso	

MLOZERA B:

FOMU YOSANTHULA NYIMBO

Mutu wa Nyimbo:			
	KUFOOKA	**PAKATIKATI**	**KULIMBIKIRA**
Kodi malemba a ziphunzitso ndi woonadi?			
Kodi malemba ali wokhulupirika ku zimene Akhristu amapanga?			
Kodi mpingo ukamvetsetsa za malemba?			
Kodi maimbidwe akulumikizana bwino ndi mawu?			
Kodi maimbidwe ndi osavuta kwa mpingo?			

ZOFUNIKA ZOVOMEREZEKA

Phunziro 1

Kuti muphunzire zambiri za tanthauzo la kulambira, onani kumene izi zikupezeka:

Mabuku:

Jeremiah, David. *Worship*. CA: Turning Point Outreach, 1995. (Onani Phunziro 1 ndi 2).

Reimers, Gary. *The Glory Due His Name*. Greenville: Bob Jones University Press, 2009.

Segler, Franklin M. and Randall Bradley. *Christian Worship: Its Theology and Practice*. Nashville: B&H Publishing, 2006. (See Chapter 1).

Zothandizira zopezeka pa Intaneti

"The Langauge of Worship: Seven Minute Seminary," At https://www.youtube.com/watch?v=RqDCG_-cbrg

"Sin and Worship in Romans: Seven Minute Seminary," At https://www.youtube.com/watch?v=6RyrW3aO0UI

Phunziro 3

Kuti muphunzire zambiri kulambira, onani kumene zikupezeka:

Peterson, David. *Engaging with God: A Biblical Theology of Worship*. Downers Grove: InterVarsity Press, 1992.

Ross, Allen P. *Recalling the Hope of Glory: Biblical Worship from the Garden to the New Creation*. Grand Rapids: Kregel Publications, 2006.

Webber, Robert. *The Biblical Foundations of Worship*. Nashville: Star Song Publishing Group, 1993.

Phunziro 5

Kuti muphunzire zambiri ya kulambira, chonde onani izi.

Segler, Franklin M. and Randall Bradley. *Christian Worship: Its Theology and Practice*. Nashville: B&H Publishing, 2006. (See Chapter 3).

Webber, Robert. *Rediscovering the Missing Jewel: A Study in Worship Through the Centuries*. Peabody: Hendrickson Publishers, 1997.

Webber, Robert. *Twenty Centuries of Christian Worship*. Nashville: Star Song Publishing Group, 1994.

Phunziro 6

Kuti muphunzire zambiri za nyimbo pa kulambira, onani izi.

Hustad, Donald. *Jubilate II: Church Music in Worship and Renewal*. Carol Stream: Hope Publishing, 1993.

Janvier, George. *Leading the Church in Music and Worship*. Nigeria: Africa Christian Textbooks, 2003.

Lloyd-Jones, D. Martyn. *Singing to the Lord*. Wales: Bryntirion Press, 2003.

Wolf, Garen. *Church Music Matters*. Salem: Schmul Publishing, 2005.

Phunziro 7

Kuti muphunzire zambiri za malemba ndi pemphero pa kulambira, onani izi.

Bounds, E. M. *Power through Prayer*. (Many editions are available).

Drury, Keith. *The Wonder of Worship: Why We Worship the Way We Do*. Fishers: Wesleyan Publishing House, 2002.

Duewel, Wesley. *Mighty Prevailing Prayer*. Grand Rapids: Zondervan, 2013.

Murray, Andrew. *With Christ in the School of Prayer*. (Many editions are available).

Phunziro 9

Stauffer, S. Anita, ed. “The Nairobi Statement on Worship and Culture,” in *Christian Worship: Unity in Cultural Diversity*. Geneva: Lutheran World Federation, 1996.

Witvliet, John D. “An Open and Discerning Approach to Culture.” Video lecture. At https://worship.calvin.edu/resources/resource-library/an-open-and-discerning-approach-to-culture

MBIRI YA NTCHITO

DZINA LA OPHUNZIRA_____

Tebulo ili mmusimu, lembanipo ngati ntchito ina yamalizika. Mayeso amakhala kuti amalizika ngati wophunzira apeza malikisi okawana 70% kapena kuposera. Ntchito yonse ikuyenera kumalizidwa ngati mufuna kulandira satifiketi yochokera ku Kalasi ya Abusa pa Dziko Lonse.

PHUNZIRO	MAYESO	NTCHITO		
1				
2				
3				
4				
5				
6				
7				
8				
9				
10				

Kulemba za zofunsa za satifiketi yoti mwamaliza maphunziro a Kalasi ya Abusa pa Dziko Lonse mukhoza kuyipeza ndi kulembera pa tsamba lathu la intaneti pa www.shepherdsglobal.org. Masatifiketiwa adzatumizidwa pa intaneti kuchokera kwa Mtsogoleri wa SGC kupita kwa aphunzitsi ndi onse oyendetsa za maphunziro amene amaliza kulemba za zofunsa za ma satifiketi m’malo mwa ophunzira.

MALEMBA AMENE AWONDEDWA

Genesis 3, 49
Genesis 4, 47, 52
Genesis 5, 49
Genesis 6, 49
Genesis 17, 49
Genesis 18, 50, 52, 53, 146
Genesis 22, 52
Genesis 28, 50

Eksodo 15, 121, 146, 168
Eksodo 19, 37
Eksodo 20, 13, 32
Eksodo 24, 47, 134
Eksodo 25, 152
Eksodo 28-29, 162
Eksodo 32, 113, 146
Eksodo 39-40, 19

Levitiko 1, 55
Levitiko 1-7, 54
Levitiko 10, 12, 48
Levitiko 19, 33

Oweruza 5, 106

1 Samueli 2, 146
1 Samueli 13, 12
1 Samueli 15, 53

2 Samueli 24, 59, 141

1 Mfumu 8, 122
1 Mafumu 18, 31, 51

1 Mbiri 29, 146

2 Mbiri 5, 55, 64, 107, 161, 164, 186
2 Mbiri 6, 144
2 Mbiri 26, 48

Ezara 9, 146

Nehemiya 8, 76, 135, 139, 143

Yobu 42, 90

Masalimo 1, 39, 76
Masalimo 8, 168
Masalimo 10, 57
Masalimo 15, 36, 37, 38, 39, 40, 41, 44, 50, 180
Masalimo 18, 144
Masalimo 19, 33, 85
Masalimo 22, 14, 33
Masalimo 24, 36
Masalimo 32, 144
Masalimo 38, 144
Masalimo 41, 144
Masalimo 42, 128
Masalimo 47, 198
Masalimo 51, 144, 146
Masalimo 66, 180
Masalimo 88, 56, 144
Masalimo 91, 121
Masalimo 95, 165, 180, 186, 225
Masalimo 96, 20, 25, 35, 122, 149, 180
Masalimo 100, 89, 104, 180
Masalimo 103, 37
Masalimo 105, 57, 180
Masalimo 107, 180
Masalimo 111, 26
Masalimo 115, 215
Masalimo 116, 144
Masalimo 120-134, 43, 54, 56
Masalimo 124, 139
Masalimo 133, 43
Masalimo 134, 43
Masalimo 135-136, 34
Masalimo 136, 57, 139
Masalimo 147, 26
Masalimo 148, 117
Masalimo 148-150, 57
Masalimo 149, 112, 180
Masalimo 150, 26, 125, 180

Mlaliki 4, 171

Yesaya 1, 59

Yesaya 6, 12, 13, 14, 15, 20, 25, 26, 33, 39, 72, 141, 147, 165, 168, 215, 227
Yesaya 29, 9
Yesaya 56, 144

Yeremiya 7, 212, 220

Ezekieli 36, 170

Danieli 6, 218
Danieli 9, 146

Amosi 5, 59, 212

Mika 6, 36, 45, 46, 65

Haggai 1, 59

Malaki 1, 12, 19, 48, 59

Mateyu 2, 13
Mateyu 4, 69
Mateyu 5, 139
Mateyu 6, 70, 133, 147, 149, 151, 160
Mateyu 9, 13
Mateyu 12, 60, 70
Mateyu 14, 13
Mateyu 15, 13, 40
Mateyu 17, 37, 84
Mateyu 18, 71
Mateyu 21, 38, 69
Mateyu 23, 70, 142, 212
Mateyu 26, 69, 107, 150, 154
Mateyu 28, 13, 77, 84

Marko 1, 71, 169
Marko 11, 69

Luka 1, 77, 146
Luka 2, 68, 77
Luka 4, 69, 135, 169
Luka 6, 69
Luka 10, 24

Luka 11, 69, 146, 147
Luka 13, 70
Luka 18, 69
Luka 19, 69
Luka 22, 71
Luka 24, 136

Yohane 2, 69
Yohane 3, 152, 170
Yohane 4, 7, 8, 9, 17, 18, 20, 22, 25, 28, 36, 68, 223
Yohane 5, 70
Yohane 17, 43, 69

Machitidwe 1, 73, 84
Machitidwe 2, 10, 11, 13, 25, 73, 76, 77, 136
Machitidwe 3, 13, 73
Machitidwe 4, 13, 73
Machitidwe 5, 12, 13, 73
Machitidwe 6, 175
Machitidwe 13, 73, 76
Machitidwe 14, 73
Machitidwe 16, 14, 107
Machitidwe 17, 18, 73, 74, 75, 87
Machitidwe 18, 73
Machitidwe 19, 72, 73
Machitidwe 20, 152
Machitidwe 26, 11
Machitidwe 28, 73

Aroma 1, 16, 25, 69, 81
Aroma 1-11, 218
Aroma 12, 10, 25, 64, 67, 87, 190, 211, 213, 217, 219, 222
Aroma 12-16, 218
Aroma 13, 219
Aroma 14, 187, 198, 200, 207, 210, 219
Aroma 16, 73

1 Akorinto 1, 11
1 Akorinto 2, 202
1 Akorinto 8, 200
1 Akorinto 10, 155, 157, 211, 212, 223
1 Akorinto 11, 13, 154
1 Akorinto 14, 77, 187, 204, 210

2 Akorinto 3, 142, 215
2 Akorinto 8, 150, 152
2 Akorinto 9, 150, 151, 152
2 Akorinto 13, 11

Aefeso 1, 146
Aefeso 4, 17, 43
Aefeso 5, 77, 109, 121

Afilipi 1, 146
Afilipi 2, 70, 71, 75, 77, 79
Afilipi 3, 35
Afilipi 4, 150

Akolose 2, 11
Akolose 3, 76, 77, 105, 107, 108, 113, 118, 121, 131
Akolose 4, 73, 76, 135

1 Atesalonika 5, 76

2 Atesalonika 1, 148

1 Timoteyo 1, 61, 125
1 Timoteyo 2, 77
1 Timoteyo 4, 76, 135, 201

2 Timoteyo 4, 76

Tito 2, 76

Filimoni , 73

Ahebri 10, 213, 218
Ahebri 13, 149

Yakobo 1, 11, 12, 25, 147, 175

2 Petulo 3, 135

1 Yohane 3, 151

Chivumbulutso 1, 78, 84
Chivumbulutso 4, 9, 20, 25, 26, 32, 33, 44, 81, 85, 107, 146
Chivumbulutso 4-5, 80
Chivumbulutso 5, 29, 33, 34, 44, 70
Chivumbulutso 11, 34
Chivumbulutso 15, 79, 80
Chivumbulutso 19, 35
Chivumbulutso 21, 80, 84

MAPETO

A

Zolengeza, 162

B

Kulinganiza mu kulambira, 56, 150–151

Kuyamba kulambira, 161

C

Kalendala, mpingo, 153

Ana ndi achinyamata, 182–183

Mgonero, 70, 137–140

Kuyimba kwa mpingo onse, 91, 97, 110

Nkhani za chikhalidwe, *Phunziro 9*

E

Zizindikiro za kulambira, 69, 87–89, *Phunziro 1*; *Phunziro 10*

Maimvaimva, 100, 184–185

Chisokole, 66–69

F

Kulambira kwabodza, 63, 67

G

Ulemelero wa Mulungu, 195

Chisomo cha kulambira, 46

M

Kusokoneza, 159–161

Chitsanzo cha kulambira (Khristu), 62

O

Kumvera, 11, 35, 48, 51, 198

Kupereka, 133–137

P

Machitidwe, 156, 187

Matamando, kulengengeza/kufokonzera, 53

Pemphero, 128–133

Kulalikira, 125–127

R

Miyambo mukulambira, 50, 54–55

S

Malemba mukulambira, 69, 122–125

Nkhani za machitidwe, *Phunziro 9*

V

Zofunikira, 194

W

Ziopsezo za Kulambira

- Kusokoneza miyambo yosinthika ndi Mfundo zosasinthika, 90
- Chinyengo, 37
- Kusalinganizika mu kulambira, 56
- Kusoweka kwa nyimbo ya mpingo onse, 97
- Kusoweka kwa Mawu, 127
- Kulambira kopanda tanthauzo, 85
- Zolowa mmalo mwa kulambira kowona, 20
- Kupeputsa kulambira, 186
- “Timachita izi chifukwa…”, 162
- Kulambira kopanda usodzi, 68
- Kulambira kopanda kumvera, 198

Mtsogoleri wa kulambira, 146, 156–159

KUFOTOKONZERA KWA MAPHUNZIRO A ABUSA PADZIKO LONSE

MAZIKO A MAPHUNZIRO A ZIPHUNZITSO ZA MAWU A MULUNGU

Zikhulupiriro za Akhristu

Izi ndi tsatanetsatane wa za maphunziro a za Mawu a Mulungu, kufotokoza za chiphunzitso cha Akhristu zokhuza Baibulo, Mulungu, munthu, tchimo, Khristu, chipulumutso, Mzimu Woyera, mpingo, ndi zinthu zomalizira.

Aroma

Maphunziro awa akuphunzitsa za chipulumutso ndi za mautumiki monga mmene akufotokozera ku Aroma, kufotokozera zinthu zingapo zimene zakhala zili zovuta mu mpingo.

Masiku omaliza

Maphunziro awa akuphunzitsa za mabuku a mu Baibulo, a Danieli ndi Chivumbulutso komanso ndi ma buku ena a uneneri ndikutsimikiza za zofunikira za chiphunzitso, monga za kubweranso kwa Khristu, chiweruzo chomaliza ndi Ufumu wosatha wa Mulungu.

Ziphunzitso ndi Machitidwe a Moyo wa Uzimu

Maphunziro awa akupereka za kufotokoza kwa baibulo kwa moyo woyera umene Mulungu akuyembekeza ndi nkulimbikitsa mkhristu.

Ziphunzitso ndi machitidwe a Mpingo

Maphunziro awa akufotokoza za mmene Mulungu anapangira dongosolo Lake pa za mpingo, zokhudza baibulo, anthu a mumpingo, ubatizo, mgonero, chakhumi, ndi utsogoleri wa za uzimu.

KAFUKUFUKU WA MAPHUNZIRO A ZA BAIBULO

Kufufuza za Chipangano Chakale

Maphunziro awa akuphunzitsa zinthu zofunikira ndi chiphunzitso cha mabuku 39 a mu Chipangano Chakale.

Kufufuza za Chipangano Chakale

Maphunziro awa akuphunzitsa za zinthu zofunika ndi ziphunzitso za mabuku 27 a mu Chipangano Chatsopano.

Mfundo za kumasulira za mu Baibulo

Maphunziro awa akuphunzitsa Mfundo ndi njira zotanthauzira Baibulo bwinobwino kuti tilondoleze za moyo wathu ndi ubale wathu ndi Mulungu.

MAPHUNZIRO A UTUMIKI NDI UPHUNZITSI

Chiyambi cha Kumvetsa

Maphunziro awa akuphunzitsa za sayansi, za mbiri yakale, ndi pa phata pa malingaliro a mmene Mkhristu akuliuonera dziko, ndikuonetsa mmene chikhulupiriro cha Mkhristu chili chofanana ndi choonadi.

Zipembedzo ndi magulu za dziko lapansi

Maphunziro awa akupereka chidziwitso kwa ophunzitsa wokhulupirira pa za kuphunzira ndi mayankhidwe abwino kwa magulu a zachipembedzo okwana 18.

Ulaliki wa mu Baibulo ndi Chiphunzitso

Maphunziro awa akupereka mfundo za mu Baibulo zimene zimatsogolera njira za ziphunzitso. Zimakamba za mitundu ya ziphunzitso ndi kupereka maphunziro ogwiritsa ntchito pophunzitsa otembenuka atsopano.

Kupangidwa kwa Uzimu

Mu maphunziro awa, ophunzira aphunzira kudziwe kukhala ndi khalidwe la Yesu, lolumikizana ndi Mulungu monga mmene Yesu analumikizana ndi Atate, kudzichepetsa monga mmene Yesu anachitira, kupanga za uzimu komanso chikhalidwe cha umunthu cha Yesu, kupilira ku masautso monga mmene Yesu anachitira, komanso kupanga limodzi ndi anthu a Chikhristu (Mpingo) amene anapangidwa ndi Yesu.

Makhalidwe Enieni a Mkhristu

Maphunziro awa amaika mfundo za uzimu ku zakagwiritsidwe ntchito ka ndalama, ubale, pa malo, ubale ndi boma, ufulu wa anthu, ndi madera ena amene akukhudza mmene timakhalira.

Ukwati wa Chikhristu ndi Banja

Maphunziro awa akupereka chithunzithunzi cha chikhristu ku chitukuko cha wanthu kudzera mu magawo a moyo ndi kuphatikizapo mfundo za mu malemba ku maudindo a pa banja ndi a ubale.

MAPHUNZIRO A UTSOGOLERI WA CHIKHRISTU

Utsogoleri wa Utumiki

Maphunziro awa akutsimikiza za chikhalidwe cha Mkhristu pamene atsogoleri akuphunzitsidwa kutsogolera mabungwe kudzera njira yodziwira zofunika, kuzindikira za cholinga, kugawana za masomphenya, kuika zolinga za kutsogolo, kupanga njira zina za masamu, kutengapo mbali, ndi kuona zomwe zakwaniritsidwa.

Moyo Ndi Utumiki wa Yesu

Maphunziro awa akuphunzitsa za moyo wa Yesu ngati chitsanzo cha utumiki ndi utsogoleri mu zaka za zino za lero.

Mfundo za Kulumikizana

Maphunziro awa akuphunzitsa za kulumikizana ndi za maphunziro a za umulungu, njira za kalankhulidwe komveka bwino, njira zokonzekera ndi kupereka chiphunzitso cha mu Baibulo.

Chiyambi cha Kulambira cha Chikhristu

Maphunziro awa akufotokoza za mmene kulambira kumakhudzira mbali zonse za moyo wa wokhulupirira ndi kupereka mfundo zimene zingatsolere munthu ndi machitidwe a mpingo polambira.

MAPHUNZIRO A MBIRI A MPINGO

Kafukufuku wa Mbiri ya Mpingo I

Maphunziro awa akufotokoza za mmene mpingo unakwaniritsira za utumiki wake komanso kuteteza ziphunzitso zofunikira kuchokera nthawi ya mipingo yakale kufikira nthawi yokonzanso za chipembedzo.

Kafukufuku wa Mbiri ya Mpingo II

Maphunziro awa akufotokoza za mmene mpingo unakulira komanso kukumana ndi zovuta kudzera munjira yochokera ku chiyambi kufikira makono ano.

Yokhazikika mwa Khristu. Maphunziro. Kulikonse.

SHEPHERDSGLOBAL.ORG